



Kubwelera
ku
chiyambidwe

*Zolankhulalidwa mosakonzekeratu monga
Mzimu afuna mudzi ndi mudzi*

Kubwelera ku Chiyambidwe

Mkwatibwi Akonzekera	3
Kuchotsa Zipupa	5
Zimathandauza Chiani Kukhala Wa Nsembe	11
Yesu Yekha Ndiye Bwana	25
Devedi Living'isitoni Ndi Mkate Ochokera Kumwamba	33
Mulungu Wa Dongosolo Ndi Aefenso 4	43
Maziko A Yesu.....	51
Nyumba Ya Mulungu	57
Mtima, Moyo, Maganizo Ndi Mphamvu.....	63
Mapelekedwe A Ndalama Mu Ufumu Wa Mulungu	73
Kufunduka Kwa Gulugufe.....	83
Zochitika Mu Dziko La Chipembedzo	85
Madziko Anayi A Choonadi	93
Kubowoleza Kwa Ulemerero	115
Mipando Isanu.....	121
Kudzadzidwa Ndi Mzimu Woyera Pamodzi!!!	137
Kudzodza Kwa Wonse Yesu Ndiye Banja.....	145
Ubatizo Wa Yesu.....	175
Kuyembekeza Pa Ambuye M'moyo Athu.....	187
Mzimu Wotengeka Tengeka	191

Mwa nthawi zonse ngati mufuna thandizo munjira ina ili yonse,
Lemberani kuno ku Mpingo Indiana,
P.O Box 68309 Indianapolis IN 46268 USA.

Kapena **www.Yesu-Kristo.com**

©2003 RealPeople@JesusLifeTogether.com
Munkhoza kuchulukitsa bukhu loseli mutafunsa kwa mkozi ndipo
mulu ndi ufulu ochulukitsa monga lili bukhuli, koma bukhuli
ndi losagulitsa pa mtengo uli wonse
(2 Akorinto 2:17 Mateyu 10:8)

Musimu muli maina a mabukhu khumi onena za maziko a ufumu wa Mulungu ndi mkwatibwi wa Yesu.
www.JesusLifeTogether.com/

NYUNDO - Kugwetsa zosamvetsetseka
Kodi mau anga safanana ndi moto? Ati Yehova ndi kufanana ndi nyundo imene iphwanya mwala? Yesaya 23:29.

WODULA - Kubyala chiyembekezo ndi masomphenya
“Taonani akudza masiku, ati Yehova akuti wolima adzapezana ndi wodula, ndi woponda mphesa, adzapezana ndi wofesa ndi mapili adzakhetsa vinyo watsopano, ndi zitunda zonse zidzasungunuka” Amosi 9:13.

MUYESO - Kugwilitsa mu mulingo wa Mulungu
Muyeso wonyenga unyasa Yehova. Koma mulingo wamphumphu umasekeretsa. Miyambo 11:1

MBIYA YOSUNGUNULIRA - Kukonza ndi kusoka mkumanizano
Siliva ali ndi mbiya yosungunulira, golidi ali ndi ng'anjo koma Yehova ayesa mitima. Miyambo 17:3

CHISENGA - Kukonza munda ndi kusintha kukolola
pakuti zipatso, pamenepo atumiza senga, pakuti nthawi yakumweta yafika Mariko 4:29.

CHOMANGIRA - Zimatengela umo mumangila!
Monga mose achenjezedwa m'mene amafuna kupanga chihema: pakuti chenjera, ati uchite zonse monga mwa chitsanzo choonetsedwa kwa ine mphiri. Ahebri 8:5.

LUPANGA - Kudula mopitilira thandwe la pansu
Musangalire kuti ndidadzera kuponya Mtendere pa dziko lapansi. Sindinadzela kuponya mtendele koma lupanga. Mateyu 10:34.

NKWANGWA - “Ndizamanga Mpingo wanga”
Ndipo nyumbayo pomangidwa inamangidwa ndi miyala yokonzeratu. Asanaitule ndipo m'nyumbamo simunamveke kulira nyundo kapena nkhwangwa, kapena chipangizo chachitsulo pomangidwa iyo 1 Mafumu 6:7.

MTOVU - Kutulutsa moyo
Taonani, ndalenga wachipala amene abvukula moto wa makala, ndi kutulutsamo kuti apasule. Yesaya 54:16.

CHINGWE CHOYESERA - Maziko oona
Ndikhamu la nkondo ai, ndi mphamvu ai, koma ndi Mzimu wanga, ati Yehova wa makamu. Ndipo adzatulutsa mwala wa chimbudzi ndi kufuula, chisomo, chisomo nao----- Pakuti wapeputsa tsiku la tinthu tating'ono ndani? Pakuti adzakondwera, nadzaona chigwe cholungamitsa chili mdzanja la zerubabele. (Zakariya 4)

Mkwatibwi Akonzekera.

September 1996, Komba, ku Africa Malawi Afrika.

Posachedwapa Yesu adzabwera kwa Mkwatibwi wake okonzekayo (Chibvumbulutso 19:7) ndipo cholinga cha Atate sichoti tidzagoonera mkwati koma kukhala mkwatibwi wake, osati kungokhala mu nyumba koma kukhala nyumba. Tingathe izi pamene tikondana wina ndi mnzake ndi kusinthana moyo wathu tsiku ndi tsiku.

Timathandizana wina ndi mnzake kudziwa Yesu bwino pothandizana kutchosa uchimo, kukondana koposa ndi kusamalilana zosowa za ena koposa zosowa zathu. Ichi ndiye chiphunzitsa cha Yesu. Umu ndiye m'mene anakhalira moyo wake kwa ife, ndipo watiitana ife kukhala motero ndi wina ndi mnzake. Umu ndi mmene mkwatibwi wakonzekera kubwelanso kwa mkwati, Yesu.

Cholinga cha Atate ndi kuti tikhale okongola koposa pamene tiphunzira m'mene tingakondane wina ndi mnzake kopambana. Pamene tichotsa kuzikonda ndi kunyada zomwe zimatinyanitsa ife wina ndi mnzake ndi pamene timatsegula moyo pofunikira kwa wina pamenepo Mzimu wa Mulungu, chisomo cha Mulungu ndi chikondi cha Mulungu chidzathilidwa pa ife----- ndipo tidzakhala mkwatibwi okongola okonzeka kubwera kwa mwamuna wathu, Yesu.

Uwu ndi mpingo ----- Wokhala motero tsiku ndi tsiku osati kuwonelera mu nyumba ya Mulungu koma kukhala malo amene Mulungu akhala nyumba zathu, kuntchito zathu ndi mpingo wathu utsakhala umodzi. Sipadzakhala zopinga mu mtima mwanga ndi wanu ndi nyumba yanga ndi yanu. Ndidzachotsa kunyada ndi kuzikonda kwanga. Ndidzachotsa ulesi ndi kusakhulupirila ndipo ndidzakonda ena monga Yesu, anaconda ine pamene aliyense atero, kuchokera wang'ono mpaka wamkulu, Yesu adzathira mafuta ochilitsa ndipo ife ndidzakhala mkwatibwi okongola.

Kuitana kwa Mulungu ku dziko la pansi

Kuitana kwa Mulungu ku dziko lonse lapansi kuti ikhale nyumba pamodzi ya Atate, mwana ndi Mzimu oyera – kukhala mkwatibwi amene wakonzekera yekha pakubwelanso kwa mkwati wake okongola, Yesu. Yohane 13:15, Aefeso 2:5, Chibvu 19:7. Yesu anati umu ndi mmene anthu adzadziwire kuti munali ophunzira anga – osati kukweza mau patsikula sabata m'mawa, osati kutha kulalika bwino osatinso misonkhano – koma “mmene mukondelana wina ndi mnzake tsiku ndi tsiku” Izi ndi zimene anthu udzadziwa kuti ndi zakumwamba. Dziko liyenela kuona ife tikukondana. Sangaone izi kufyola mu za chipunda kamodzi pa sabata ai. Ndiponso ndi zobvuta kukondana mu chipinda. Adzaona kuti timakondana pamene timatengelana katundu, pamene tisamalilana zinthu zathu. Pamene anthu onse adzadziwa kuti muli ophunzira anga – osati pa zomwe timakhulupilira koma pamene aona kuti tili okondana. Uwu ndi kuitana kwa Mulungu lero kwa anthu ake.

Kumanga pa Thandwe

Kumanga pa thandwe ndi kuchita mau ake. Mukamva zimene Yesu anena, chitani zimenezo lero. Chitani kanthu ndithu, Lero, kusintha kwa Yesu osangoganizira chabe izi. Chitani pa ichi, osati kumva chabe ophunzira a Yesu chitani izi! Choncho abale ndi alongo khalani mpingo ku ulemerero wa Mulungu. Khalani banja pamodzi tsiku ndi tsiku. Yesu akondwera nanu.

Kuchotsa Zipupa

Mzuzu Malawi ku Afrika 1996.

Mudziko limene tikhala monganso maiko ena onse thupi la Yesu lagawidwa gawidwa zidutcha. Pali zambiri zachitikira choncho kuti thupi la Yesu liphwanyike moipa nthawi zina ndi chifukwa cha kuzikonda ndi kuziyeneleza kwa anthu ena mwananso ziphunzitso zimakahla zosiyana, ndipo anthu amagawanika chifukwa pa chiphunzitso kwa nthawi amayambana ndipo amasiyana.

Ndi cholinga chinthu ndi ntchito kwa Yesu kuti tichotse makoma amenewa ndi zotsingazi. Yesu akufuna kuti thupi lake likhale limodzi dziko lonse lapansi. Pali zina zimene zifunika kusintha kuti zimenezi zichitike, ngakhale kuzikonda ndi kunyada kuchotsedwe pa ife. tiyenela kubwela pamodzi kuti tidziwe ziphunzitso za Yesu – pamodzi, osati mosiyana tiyenera kukhala ofewa ndi ozichepetsa kuphunzira kwa wina ndi mnzake.

Mwazina zimene thupi la Yesu lagawidwa ndi kufuna kwa anthu kuika maina pa Mpingo. Pamene tiyankhana mu Baibulo lokha, pamenepo sitiona kuti mpingo woona sunakhale ndi dzina ai ndithu, Palibe mpingo wa Babatisiti mu Baibulo kapena Apostoliki kapena Mpingo wa Nazarene kulibe kumeneko. Palibenso amannoncite” kapena makalazamatiki” ulipo thupi la Yesu lokha.

Pamene muwelenga za mpingo mu Baibulo amadziwika ndi maina ambiri. Koma sizikwangwani ai, Si undindo. Mpingo angakhale mpingo wa Mulungu kwa Akorinto unatchedwense oyamba kubadwa ndi chimodzimodzi. Ungatchedwense osakhidwa kapena oitanidwa. Ndi mpingo womwense kwa Akorinto. **Maina onsewa amadziwika nawo kuti anali iwo osati chizindikiro chobvalidwa.** Mwa chitsanzo ngati nditanena mbale Henry chingakhale chizindikiro ndipo ndikati Henry, mbale wanga okondedwa ndiye kuti maonekedwe, osati chizindikiro. Mipingo mu Baibulo imatchedwa ndi mawonekedwe koma osati ndi zizindikiro. Palibe pamne mu Baibulo mpingo udziwika ndi chizindikiro. Mpingo wa Babatisiti ndi chizindikiro cha chipembedzo. Abale mwa Kristu

ndi mawonekedwe. Babatisiti ndi chizindikiro. Izi ndi zimene zatigawa ife tonse muzidutcha – zidutcha. Chifukwa ngati muli ndi chizindikiro chosiyana ndi changa, ndizimene zatisiyanitsa ife tonse.

Simuli mphamvu mu mwazi wa Kristu? Tisiyane chifukwa cha maina chabe? Mufunanso dzina lina pambali pa dzina la Yesu? Palibe dzina lina m'mwamba kapena panso pano limene anthu angapululumutse nalo. Sitifuna kutchedwa ma Babasititi kapena mamone kapena Apostoli kapena Asabata. **Tiyenera kukhala okonda Yesu ndi okondana.** Ndi zokwanira MULI mphamvu mu mwazi wa Yesu. Ndipo palibe chimene chingatilekanitse. Ngati pali kusiyana pakati pa inu ndi ine ndi chifukwa choti wina wa ife safunana kukonda ndi kumvela Yesu. Ndizimene zingatisiyanitse koma ndi zokhazo zimene zingatisiyanitse kuchokera kwa mbale. Ngatyi muli ndi chizindikiro cha Babatisiti ndi ine cha sabata ndiye pali mgawikano pakati pathu umene ukukwiitsa Yesu. Ngati tikhala moyo wathu pamodzi ndi kusamalira wina ndi mnzake popanda chizindikiro cha babatisiti kapena a sabata ndiye pamenepo pamodzi tidzaphunzira kukonda Yesu, koma ngati tili zizindikiro zosiyana sitingakhale PAMODZI.

Dzina la Mpingo Wako ndi Chiyani?

Muchifuniro cha Yesu okonedwa, sitienera kukhala ndi zotchinga. M'mene Paul adalankhulira. *“Atembeledwe wina aliyense osakonda Ambuye”* tisakhale ndi matembelero tiyenera kuchotsa zotchinga zonse zazipupa, zotchinga ndi zizindikiro ndiye ngati pali mpingo mu mzinda wanu ndi mphamvu ya mwazi wa Yesu ndiye tidzakhala a Kristo pamodzi popanda maina. Mpingo umene tili takhala kokwanira zaka makumi koma ulibe dzina. Zoono ndi zoti pamene wina atifunsa “Dzina la mpingo wanu ndi chiyani? Timati, “timakonda Yesu” ngati ali a Babatisiti ndiye palibe zipupa sangaliza za ine monga mpikisano ndipo ndimaitana kuti tidzaone Yesu tonse pamodzi popanda zizindikiro.

Pamene wina afunsa mmodzi mwa ana athu “umapita ku mpingo uti” sakwanitsa kuyankha pokhapo ponena kuti “onse amene ndimawadziwa amakonda Yesu ngati wina afunsa, mumapita kuti ku mpingo? Ana athu amati “mukuti chiani? Iwowo ali mpingo tsiku ndi tsiku sanaonelera

zochitika mu mpingo. Ndife mpingo ndipo anawo amadziwa mmumtima wawo ngakhale ali ochepera msinkhu.

Ndi zofunika kuti tisakhale ndi chizindikiro mu moyo wathu. Zimafunika kuyambira ndi inu ndipo ndi onse amene mwafikire mu dziko la chipembedzo. Apempheni choonde asakhale ndi zipupa ndi zotchinga ngati muli mphamvu mwa Yesu, tisdakhale ndi zipupa, kukhala ndi maina amene mulibe mu Baibulo zimachititsa zitchinga. Anthu ena amati, koma dzina lathu lili mu Baibulo mpingo wathu amatchedwa mpingo mu Akorinto umatchedwa mpingo wa Mulungu ndiye tili ndi dzina limene lili mu Baibulo. Sikuganiza kwabwino kutero chifukwa Paulo samatchula mpingo ndi chizindikiro zimene adanena ndi zori uwu ndi mpingo umene uli wa Mulungu. Osati “Mpingo wa Mulungu mu Akorinto” koma kuti anthu a Mulungu okhala mu mzinda wa Akorinto unali mawonekedwe osati chizindikiro ndiponso anatchula anthu omwewo ndi maina ena awiri kapena atatu. Chifukwa ndi mawonekedwe. Alipo maina ambiri a mpingo koma ngati tikhala ndi dzina limodzi ndikukhala ndi dzinalo tapondeleza pa mwazi wa Yesu chifukwa tapangitsa kuti pakhale kusiyana pakati pa ife ndi ena amaene akonda Yesu. Ngati muli ofuna, yankho labwino pamene wina afunsa inu, “Dzina la mpingo wako ndi chiani? Nenani “ndimakonda Yesu” umakonda” limeneli ndiko kuyankha kwabwino. Pamene palibe zosiyana kuti wina sakonda Yesu. Iyi ndi njira ya Mulungu ndi njira ya Baibulo. Siosiyana ndi maina. Monga ananena mtumwi, Ana ang'ono inu. Kondanani wina ndi mnzake ndizimene timapanga sititenga kunyada mu mpingo mwathu, koma kwa mwamuna wathu Yesu Amen?

Wina amene ndinamdziwa amalankhula ndi “Abusa” ndipo abusawo anakhumudwa pamene anauzidwa kuti anali mpingo. Mbusawo anali kuganiza za “mpingo” umene umapita lasabata m'mawa mu nyumba yomangidwa ndiye pamene wina afunsa inu kuti ndi mpingo uti uli? Ndipo mufunsi Mulungu kupatsa nzeru momwe mungayankhire funsolo. Pakuti pali mayankho ambiri. Mukawelenga mu chipangano cha tsopano muona kuti okhulupilira mayankha munjira mosiyana, chifukwa anali m'mene mungayankhire mafunso. Mulungu adzakuonetsani pa zimene mungayankhire. Koma mukakhala ndi chizindikiro ndipo akakufunsi “muli mu mpingo uti?” muli ndi yankho limodzi lokha – chizindikiro tsopano ngati mulibe chizindikiro mungabweretse pafupi

ndi kwa Yesu powauza kwa iwo za Yesu ali ndi moyo ndi thupi lake ndi mpingo sichimene upitako, ndi chimene uli ndi Banja osati bungwe mungathe kutero pamene wina afunsa muli mu mpingo uti – pokhapo muli ndi chizindikiro chifukwa ngati sakhulupirira inu adzaganiza muli monga m’modzi amene amapita ku nyumba zomangidwa ngati musiyana mu chikhulupiriro ndi zimene amachita iwo, koma ngati mulibe dzina monga mipingo ya m’baibulo imene inalibe dzina lirilonse ndiye akafunsa dzina la mpingo munganene za banja lodabwitsa la thupi la Yesu ndi moyo wamoyo ukhala mwa anthu ake.

“Mundondomeko chikhulupiriro” - Chotchinga china

Chifukwa china chimene kuli zipembedzo ndi kuzikonda kwa anthu china ndi kusiyana kwa maonekedwe. Kusiyana kwa zotsatira mu chikhulupiriro pamene mbusa ndi munthu uja ndilankhula kale anayamba kulankhulana samadziwa zimene mnzakeyo amakhulupirira ngati munthuwo ndi abale ena adakadziwa bwino munthu winayo anakatha kulankhula zina zosiyana mukuchokera mu mgwilizano wawo. Anakatha kulankhula kubadwa kwa Yesu komanso muimfa yake ndi kuuka kwa Yesu; komanso zoti ali kubweranso kw aanthu ake. Adzayamba kuyankhula kuti Mkristu ndi ndani? Kutu ngati sungataye moyo wako kwa Yesu sungathe kumpeza iye, komanso ngati sungatenge mtanda wako sungathe kukhala ophunzira wake. Mu mgwilizano angayamba kugwira ntchito kuti mndondomeko ya chikhulupiriro ndi otani.

Muli ndi ana ndi amai? Ndongomeko ya chikhulupiriro chanu ndi yotani mu banja lanu? Pali zambiri zimene zili zofunika mu banja lanu koma mulibe mndondomeko wa chikhulupiriro m’banja lanu. Inde zimatero koma osati motero sumaika pa chipupa koma zimakhala mu mtima wanu ndi m’mitima ya ana anu chifukwa munawaphunzitsa iwo ngati ndabwera pa nyumba yanu kudzakhala ndipo simundiuzwa iwe za “ndondomeko ya chikhulupiriro” ndidzaona pa nkhope yanu. Ndidzaona m’mene mumatchalira ndi akanzi ndi ana anu ndidzaonanso m’mene mumalimbikira ntchito ndipa chakudya pagome ndipo ndikakupezani kuti mwapinda mabondo anu ndi kupemphera pa mbali poterosimunaikize muzipupa koma ndondomekowo ulipo ndithu.

Pamene mpingo ukhala banja ndi zofanana motere sitiika zinthu mu zipupa, koma pamene mwatidziwa ife mumaona mu mitima. Ngati wina adzakhala mbanja lathu, mpingo wathu (umene uli ndi anthu zana la anthu). Ndipo sakhulupirira zakubadwa kwa Yesu ndikuti iye ndi mwana wa Mulungu ndikuti mwazi wa Kristo ndi umene unatiombola ife kuchokera kumachimo, sitingawapatse ndondomeko ya chikhulupiriro chifukwa ndife banja silimodzi lokha monganso banja silikhala limodzi lokha koma chifukwa tili nawo mi mitima yathu, monga mmene banja licherira. Sipapita nthawi tisanakambilane zinthu zofunika.

Bvuto lokhala ndi ndondomeko wa chikhulupiriro ndikuika pa chipupa ndi zofanana kukhala ndi dzina la mpingo. Zimamanga zipupa ndi zotchinga pakati pa anthu, ngati munthu angabwere kwa ine, nati “ndina mbabatisiti? Ine nditi, inde ndine mbabatisiti adzaganiza kuti amandidziwa, koma sandidziwa koma zimene adziwa ndi zimene mubabatisiti amachita ndiye kumaganiza kuti amandidziwa. Mwa ichi ngati ndili mkristu opanda chizindikiro ndiye sadzaopa ine chifukwa adzaganiza kuti wandidziwa kale tsopano adzalankhula kwa ine kuti ndine ndani chifukwa sindinabisare mu chizindikiro cha Babatisiti adzalankhula kwina zazinthu zina – monga mwazi wa Yesu ndipo ndingamuuze m’mene ndimakhulupirira ngati ndikulakwitsa angathe kundithandiza kusintha koma ngati ndili wa Babatisiti amanenatu kuti “chabwino” pamene tilibe zotchinga pamenepo tidzakhala ndi mulumikizo umene tingathandize wina ndi mnzake.

Kukonda anthu, koma mudane ndi zosakaniza

pamene mpingo mu Baibulo suli ndi kugawikana pa dzina posiyanyitsa kudziwika ndi aKristo a mu mzinda wina pali chinthu ichi monga mwa mpingo pa wokha ndikunena ichi chifukwa ndi chofunika kukhala mu ubale ogwilizana ndi wina ndi mnzake. Mu dziko la Amerika pali kapena mitundu itatu pazochitika mu dziko la chikristu. Loyamba ndi mbali ya chipembedzo chokhala ndi chizindikiro. Alipo anthu abwino mu chipembedzo zimenezi ndi ena oipanso. Pali anthu amene anachoka mu chipembedzo koma sanathe kupeleka moyo wawo kwa okhulupirika ena ndipo pali kutayana. Amakonda Yesu ndipo amakhulupira choonadi koma amafuna anthu nthawi iliyonse. Malembo amati dandaulilanani wina ndi mnzake tsiku ndi tsiku pamene patchedwa lero. Ndipo

ngati sitidandaulilana wina ndi mnzake potchedwa lero. Ndipo ngati sitidandaulilana wina ndi mnzake potchedwa tsiku ndipo tidzaumitsidwa mtima ndi kuunitsidwa (Ahebri 3:12-13).

Pali ena amalowana mukulumikizidwa pamodzi tsiku ndi tsiku mu moyo. Sali mbali ya chipembedzo, koma amakonda anthu a chipembedzo. Amakonda tsiku ndi tsiku ndipo ali mpingo. Sangoyenda chisawawa ali amene Baibulo amati “olungamitsidwa pamodzi ndi mitchempha” pamene mbali ina yafooka, onse amafooka. Pamene mbali ina pali mdalitso, onse amakondwera amaima ndi kukhala pansu ndi kulankhula onse pamodzi. Uwu ndiwo mpingo opanda dzina ndi zinyumba zomangidwa kapena kuwonelera ndipo mamembala ake ali mu moyo kukondana wina ndi mnzake tsiku lililonse.

Ndiye magulu atatu amenewa. Ambiri amapita mumachitidwe otere nthawi zambiri. Ambiri tinaonetsedwa kwa Yesu mwa chipembedzo, ndipo zabwino zabwera kuchokera mukutero. Chifukwa ambiri ndi ofewa kuganiza kwawo amaona kuti sangathe kupitiliza mu chipembedzo. Yesu anati ndidzalavula otentha chabe mkamwa mwake. Muchipembedzo muli anthu otentha ndi ozizira. Pamene musakaniza kutentha ndi kuzizira ndipo amene amaganiza monga Yesu adzakhala ndi zobvuta pamene akhala ndi machitidwe otere. Tingakhala umasuka ndi kusatsaniza ngati ndife osalumikidwa ndi Yesu chifukwa iye sakonda kusakaniza. Ndipo timakhala ndi zobvuta. Timakonda anthu, timafuna kutumikira ndi kuthandiza ndiponso timawafunanso. Koma pamene pali kusakaniza sitidziwa tidzachitanji. Anthu ena amachoka muzimenezo. Kapenanso amachotsedwa, amachoka mokhumudwa ndipo ali paokha. Timafunsakuti akhale ndi anzawo mofulumira mu moyo wa tsiku ndi tsiku ndikusakhala paokha nthawi yayitali. Tiyenera kupemphera zipembedzo ndi anthu apadera-dera amaene ali kumeneko, koma zipupa ziyenera kugwetsedwa ndi kutentha chabe kuyenera kutha. Malemba anati kuchotsa chotupitsa mkate. Ichi ndi cholinga chathu – kuthandiza kuchotsa chotupitsa.

Zimathandauza Chiani Kukhala Wa Nsembe

Kuchita Zinthu mu njira ya Yesu

Mzuzu, Malawi, Africa, 1996

Popanda maudindo – ndife tonse Asembe.

Mu bukhu la Chibvumbulutso limati Yesu anatigula ife kukhala ufumu wa nsembe kutumikira Mulungu wathu (Chibvumbulutso 5) ngati tonse tingakhale ansembe tiyenera kudziwa kuti kukhala wansembe ndi chiani ngati tikufuna kukhala ndi mphamvu m'moyo mwathu tiyenera kukhala ndi maganizo a Mulungu pamoyo yathu. Yesu anati “pitani ndipo ndidzakhala nanu” Anatiphunzitsa, chitani chifuniro changa ndipo ndidzakupatsani inu moyo ndi mphamvu.

Chikristo chonama kwa nthawi yaitali chapondeleza anthu pansu. Zatengera anthu ochepa ena ndi kuwakweza ndikuwapanga Atsogoleri olemera ndi otchuka ndi a mphamvu, potero ndikupondereza ena pansu, ku America, India, Poland, Romania, Brazil ndi malo ozongulira kuli akhristu apa mwamba ndi apansi. Izi ndi zoipa. Yesu ananena kwa Atumwi khumi mu Mateyu 23 musamutche wina Mphunzitsi, musamutche Atate, musamutche wina mtsogoleri win aAmbuye, kapena (Rabbi) mphunzitsi kapena Mbusa kapena a Reverendi.

Pakuti muli nonse abale ndi Atate m'modzi palibe otchuka mu Chikristo choona koma Yesu yekha. Pasakhale mabwana olemekezeka amene akuchita zonse pa okha, ndalama, ndi anthu omwe pokhapo Yesu mwa anthu ake mwa Mzimu wake.

Nsembe ya Moyo

Pamene Mulungu afuna kuti ife tikhale ansembe anali ndi malingaliro mu maganizo ake. Wansembe amapeleka nsembe zauzimu kwa Mulungu. Mungathe kutero ndithu. Mulungu afuna kuti mutero. Sizaiwo utchuka

okha ai ndi zawina ali yense wa ife. Nsembe ya uzimu monga Paulo ananena ndi kupeleka matupi athu monga nsembe ya moyo. Yesu amafuna lilime, maso anu ndi makutu. Amafuna maganizo anu, manja ndi mapanzi. Mungathe kupeleka ziwalo zathupilano monga zida za chilungamo chokha. Kapena mungapeleke ku uchimo, kuzikonda, kunyada, chilakolako ndi mantha. Koma Yesu amafuna ife kupeleka ziwalo za thupi lathu monga nsembe tsiku lililonse ndipo tidzakhala ansembe.

Ambiri amadziwa mbali iyi yoyamba ya unsembe kupeleka thupi monga nsembe. Anthu ambiri saatha izi ai, koma ambiri amadziwa zimenezi kodi mudzachita?

Kutumukira anthu ndi kuthandiza wina ndi mnzake kukhala Yesu!

Ntchito ina pambali ya unsembe mu chipangano chakale zimene anthu ambiri sadziwa ndi kutumukira anthu – osati kupeleka nsembe zopsyeleza kokha koma kutumukira anthu. Ansembe mu chipangano chakale amabweletsa Mulungu kw anthu. Tsopano, mu chipangano chatsopano ife tonse ndife ansembe ngati muli otsatira wake wa Yesu ndinu wansembe. Sitingokhala ndikuona wansembe alikuchita ntchito ya Mulungu. Ndife a nsembe mukhulupilira mumtima mwanu kuti ndinu wansembe? Bweletsani Mulungu kwa anthu. Pali njira ziwiri zomwe mungabweletsere Mulungu kwa anthu ina ndikuwauza anthu za Yesu kwa okhala nawo pafupi. Ndife tonse ansembe, choncho timabweletsa Yesu kwa okhala nawo pafupi ndi anzathu ndi mabanja awo Amen?

Wansembe amabweletsanso Yesu ku banja la Mulungu timawauza anthu ena za Yesu ndi njira zake, koma pali njira imene timabweletsa Yesu kwa anthu. Lolani ndilankhula mu zodziwika ngati muli wansembe mudzathandiza ena kukhala ngati Yesu. Ngati mungaone chithunzi cha Yesu mu mtima wanu ndi kuona kuti ali otani, ndiye yang'anani mlongo mbale amene ali ndi inu ndikaona kusiyana kwawo ndi Yesu ngati ansembe timafanitsa kukhala otero ndi iye. Kodi Yesu ndi ozikonda? Mbale wina kapena mlongo ozikonda? Inu ndinu wansembe, athandizeni, mudzathandiza ena. Kodi Yesu amaopa? Mbale wina kapena mlongo akamaopa, athandizeni kodi Yesu amasalila ana? Kodi anati

“Bweletsani ana adze kwa ine? Ngati muona mbale, mlongo amene sakonda ana ang'ono ndi kuwasamala, ndiye thandizani kusintha ndi zimene wansembe amachita. Timathandiza aliyense kukhala monga Yesu ali ngati Yesu anakakwatira anakakhala okwiya ndi ukali kwa mkazi wake? Ngati Yesu anakakhala mkazi anakakhala okwiya kapena kuzikonda kwa mwamuna wake? Mudziwa mayankho ake ku mafunso amenewa Yesu odabwitsa mu zinthu zonse.

Inu ndinu ansembe thandizani abale ndi alongo kukhala monga Yesu analiri. Izi ndi zopweteka, izi ndi zobvuta. Chifukwa wina adzaganiza kuti muli woziyeneleza kapena oweluzu chabe koma ai, inu ndinu wansembe monga wansembe monga Mulungu wakuitanilani. Sitifuna kukhala wozikonda kapena woweluzu chabe. Tikufuna kukhala ozama, kuzama mu chikondi mu mtima yathu kwa aliyense. Koma tiyenenla kwafunsa kusintha kuti akhale monga Yesu – chifukwa ife ndife ansembe a chifumu.

Aliyense waife ndi wansembe wa Mulungu. Koma ndili ndi mabvuto athu ameneyonso, zilipo zinthu zimene aliyense waife sakwanitsa monga Yesu ngati ndikhulupilira kuti muli wansembe, ndiye ndiyenera kumvera kw ainu kuwona zinthu pa moyo umene sulingana ndi Yesu.

Ndikuitaneni inu monga wansembe kuona mu moyo ndi kuthandiza ena. Tili ndi kulimbika ndi kuzichepetsa pofuna anzathu kutithandiza ndikulankhula ndi moyo wathu. Mpingo sikumalo amene umapita ai mpingo ndi anthu pokhala ansembe pamodzi, umakhala mpingo pamene aliyense akuthandiza wina ndi mnzake tsiku ndi tsiku kukhala monga Yesu. Simuli mpingo chifukwa muli pena ndipo mukumvera. Ndinu mpingo umatchedwa thupi la Kristo.

Ngati sitithandiza ena kukhala monga Kristo ndiye kuti sitili kumbali ya thupi lake. Tiyenera kuthandizana wina ndi mzake.

Atate, woyera Ambuye Mulungu wa mphamvu, ndi pemphero tonse pamodzi kuti mutsegule maso athu ndi ana onse kulikonse. Mulungu woyera, tionetseni kwa ife mmene tingakhali ansembe. Tipempha inu pakulimbika, kuthandiza ndi nzeru zimene zingakhudze moyo wa ena. Tikupemphani mu kuzichepetsa ndi kulimbika polora anthu ena kulankhula ndi miyoyo yathu.

Tikufunani kwambiri, tifuna kukhala mpingo wanu. Tifunanso kugwetsa makomo a ndende ndi kukondana wina ndi mzake mwa pamwamba. Mzimu woyera, thandizani ife. Phunzitsani ife njira zanu, thandizani ife kusintha mofulumira. Tikukondani koposa. Tipatseni ife nzeru yanu. Tidziwa kuti nyumba yanu imangidwa ndi nzeru, ndipo tifuna koposa. AMEN.

Kuthetsa Mabvuto

Ndipo ngati mbale wako akuchimwira iwe, pita mulangize pa nokha iwe ndi iye, ngati akumvera iwe, wambweza mbale wako. Koma ngati samvera, onjeza kutenga ndi iwe m'odzi kapena awiri kuti atsimikizidwe mau onse pakamwa pa mboni ziwiri kapena zitatu. Ndipo ngati iyee samvera iwo, uuze mpingo, ndipo ngati mpingo ngati iye samveranso mpingowo, akhale kwa iwe monga wakunja ndi wamsonkho. Indetu ndinena kwa inu zilizonse mukazimanga padziko lapansi zidzakhala zomangidwa kumwamba ndipo zili zonse mukazimasula pa dziko lapansi, zidzakhala zomasulidwa kumwamba. Ndiponso ndinena kw'ainu kuti ngati awiri a inu abvimerezana pansu pano chinthu chilichonse akachipempha, Atate wanga wakumwamba adzawachitira. Pakuti kumene kuli awiri kapena atatu asonkhanira m'dzina langa ndili komweko pakati pawo. (Mateyu 18- 15-20)

Anthu ambiri amene amamva vesi 20 amaganiza ndi pamene mpingo wonse ukumana ndi pamene tili okondwa kuti Yesu ali pompo. Timaimba matamando kwa Yesu, timamva bwino ndi kumva kupezeka kwakwe. Pamene zimenezi zili zoonza sizimene Vesi 20 limanena ndime imeneyi. Sinena za anthu kukhala pafupi ndi kuti Yesu ali pakati pawo, koma salankhulanso za kulambira pano. Akulankhula kuthetsa mabvuto. Akuti pamene tili ansembe ndikuthandiza ena monga Yesu ali pali nthawi imene timayenera kubwela mu moyo wa aliyense. Mukaona ine kuzikonda muyenera kubwela ndi kundiuza. Pamene mlongo wina aona mlongo wina akunena za wina. Mulankhuleni za zimenezi. Mjedo ndi chimo, mjedo umaswa mtima wa Yesu. Njedo ndi mwano ndi umapweteka Yesu ndiye pamene taona kuti ndi uchimo ndipo labvulaza Yesu mu thupi lake, monga wansembe ndi thupi la Kristu. Tiyenera kuthandizana.

Yesu anati ngati pali utchimo muyenera kupita kwa iyeyo basi (ndime 15) sitifuna kuchititsa manyazi ena. Mu chikondi timafuna akhale monga Yesu,

ngati ali wozikonda kapena a njedo sangathe kumva Mulungu. Pokhala ndifuna kuti amve Mulungu, Tiyenera kuthandiza ngati ali wonyada kapena kuzikweza ndi a mwano, mdiye sangakonde Mulungu kapena Anthu mwabwino. Choncho monga Ansembe tiyenera kupita kwa iwo kuti akhale monga Yesu. Koma, tiyenera kuzichepetsa. Sitikuloza chala ndi kuloza tagwira miyendo yawo ndi kuwapempha kuti apelikeye moyo wawo kwa Yesu. Tikufuna iwo kuti akhale pa ubwenzi ndi Mulungu ndiye sangathe kutero ndi Mulungu ngati pali tchimo mu mitima yawo, ndiye Ambuye ndi Mphunzitsi Yesu amati tipite kwa iye yekha. Musachititse manyazi kapena kuwauza iwo akondeni. Koma pitani kwa iwo ndi muwathandize ndinu wansembe, mupite.

Ngati awiri kapena atatu ndi enanso Yesu amabwelanso, pomwepo!

Yesu amapeleka mayankho ku mabvuto pamene zinthu zabvuta. Pamene tapita kwa mbale kapena mlongo mu kuzichepetsa kuyesela kuzichepetsa ndi kunena kuti, chokani, sindifuna kumva kapena osandiweluzi ine. Chotsani chitsotso mu diso lanu. Yesu amapeleka yankho pabvuto ili. Pali mbali yoti mungalakwe koma muyenerabe kupita ngati mukuganiza kuti sindinu olakwa. Yesaniso ngati mukuopa kuyesa, ndiye sindinu wansembe. Simungakondweletse Yesu ngati mpaka mutayensa. Mwina mwalakwitsadi choncho ndi bwino kutero, chifukwa adzaphunzilanso pa ichi Yesu anati ngati mukupita kwa mbale kapena mlongo ndiye samvera, tengani awiri kapena atatu kuyesela kuthandiza. Ichi sichiphunzitsa cha “makhalidwe a mu mpingo” Ichi ndi chiphunzitsa cha mmene tingathandizire wina ndi mzake.

Pakuti kumene kuli awiri kapena atatu asonkhana mdzina langa, ndilikomweko paka ati pawo. (Mateyu 18:20)

Pamene pali awiri kapena atatu asonkhana pogwira ntchito yake, Yesu amabwera. Malembo awa sinthawi ya kulambira. Uku ndi kugwira ntchito pamodzi kuthandiza ena kukhala monga Yesu. Ngati tipita kwa mbale kapena mlongo, ndipo sakumvera chifukwa sakumvetsa kapena kufuna izi, pamene tibweletse abale awiri kapena atatu ena tonse. Ili ndi lamulo la Yesu. Sanati ngati samvera inu muiwala kapena kupempha.

Anati ngati samvera inu, tengani awiri kapena atatu alongo kapena abale, ndipo Yesu adzabweranso.

Ngati tibwera mu dzina lake pochita ntchito yake. Iye adzabwera ndi kuthandiza. Ananenanso kuti ngati iye samvelanso awiri kapena mboni zitatu. Ndipo uzani mpingo wonse. Kenanso, ichi “simakhalidwe a mu mpingo” ichi ndi kubweletsa ansembe pamodzi kuyensa kuthetsa bvuto. Zimenezi ndi zabwino.

Yesu wathu ndi wanzeru zosawelengeka. Iye ndi wauphungu wodabwitsa sichoncho kodi? Yesu anati kuti ngati pali mabvuto bweletsani ansembe kuyesa kuthandiza wina ndi mzake, tingabweletsenso anthu ena kudzathandiza, ngati ndibwera ndikuona kuti pali tchimo mu moyo ndipo simubvomeleza, poti kapena ine ndalakwitsa – kapena sindiona zinthu bwino. Pamene tibweletsa awiri kapena mbino zitatu mwina adzanena kuti ndalakwitsa. Choncho Yesu amapambana, ndi onse amakula. Izi ndi zopambana kuzidziwa ngati muli Ansembe. Zinthu siziyenda bwino nthawi zonse, koma tiyenela kukhala ndi kulimbika ndi chikondi. Tiyenera kumvera Yesu mu zimene anena nafe pamene zinthu sizili bwino. Ngati zinthu sizingayende bwino titenge anthu ena ndi kumvera pamodzi Yesu. Nthawi zina munthu m’modzi amakhoza mwinanso winayo ndi okhonza. Ndi nthawi zina onse ndi okhonza ndipo zimakhala kusamvetsana bwino. Mwinanso onse ndi olakwa, koma akamvela malamulo a Yesu pobweletsa awiri kapena atatu – ngati timvela kwa Yesu ndipo tisamalitsa – pamene Yesu adzabwera kudzathetsa mabvutowo ndi kutithandiza.

Chida chodabwitsa

Wamkulu wa nsembe adzathandiza ansembe onse, koma tiyenera kuchita mu njira yake osati, ulesi posalankhulitsana kwa wina ndi mzake. Tisachite mantha kubweletsa ena ndi kulankhula za izi ndipo ngati wina wabwera kudzalankhula nafe. Chifukwa ndimakonda Yesu ndi choonadi, ndipo ndaona kuti ndachimwa. Kuitana ena kuthandiza ndi kuonetsara kudabwitsa mu nzeru ya Mulungu. Ndidziwa kuti ngati awiri kapena atatu ena abwera. Yesu amabweranso.

Monga Ansembe, tiyenera kuganiza za izi ndi kuziika mu ntchito. Simasewero chabe sitikuyensa kukwanitsana wina ndi mzake pamene

tikubwelerera polankhulana nthawi zonse. Sikuti taikidwa ngati a polisi. Koma ndi kukondana wina ndi mzake mokwana ndi kuyensa kuthandiza. Pamene pali uchimo makutu amakhala otseka pakusamva Mulungu. Pamene pali uchimo maso amakhala osaona Mulungu ndiye monga ansembe tiyenera kuthandizana kumva Mulungu ndi kuona Mulungu pothandiza kuchotsa chimo.

Yesu anatipanga zida izi mu zoikira zida ngati sitingathese mabvuto amodzi ndi amodzi. Pamene pamene anatipatsa ife zida zobweletsa ena kuthandiza kuthetsa zobvuta. Uwu ndiye ukwati weniweni ngati akazi anga ali ndi bvuto ndi ine ndipo sindikumvera, ndikudikira kuti amvera Yesu ndikubweletsa awiri kapena atatu ena. Yesu, sananene kuti zonse ndi zotero koma mu ukwati ai. Iye anati zonse ndi zoonza kwa anthu onse okhulupilira. Zonse ndi zoonza kwa ansembe onse. Ngati akazi anga aona uchimo paine ndipo sindikumvera ayenera kutenga awiri kapena atatu ena. Ndifuna iye atero, chifukwa ndikonda Yesu ndi zimene wina wa inu afuna? Izi ndi zolimbikitsa.

Landilani mpeni muchilitsidwe.

Nthawi zonse, mpeni umapweteka, koma Yesu ndi sing’ang’a wamkulu amachotsa khasa kuti tikhale wabwino ndi mphamvu. Zimene talankhulazi ndi zopweteka pang’ono nthawi zina, koma mukamvera njira ya Yesu ndi kuzichepesa ndi kukonda ndiye adzakupangani inu a mphamvu ndi nzeru ndi wopambana. Adzachelitsa nthenda zathu zonse za mu mtima ndi thupi. Adzaika chikondi chozama mu mtima ndi kukupatsani moyo mudzakhala mitsinje ya moyo yotuphuka kuchokera mwa inu ndi Mtendere zimene zidutsakudziwakonse. Mudzakhalandi chimwemwe chosaneneka chodzadza cha mu ulemmerero. Mudzakhala ndi mphamvu ya moyo wa ngwiro, ngati mudzachita mu njira ya Yesu ndikukhala ansembe simudzakhala anthu chabe. Mudzakhala ndi kudzadza kwa mzimu woyera ndi nzeru koma muyenera kulandira mpeni podula uchimo wonse. Muyenera kukhala okonzekera mpeni kudula chimo. Mukhale okondwa pothandizidwa, ngakhale pamene zipweteka uwu ndi maganizo a ophunzira wa Yesu.

Aliyense angathe kukhala mu chinyumba ndi kumvetsera mau onse. Koma Yesu watiitana ife kukhala ansembe ndi mafumu. Paulo anakalipira abale

akwa Akorintho pamene anati “mulikuchita ngati anthu wamba monga adziko la anthu” koma Mulungu watiitana ife kuweluzza angelo, watiitana ife kukhala odzadza ndi moyo ndi ulemerero ndi mphamvu monga mwana wake, Yesu. Koma tiyenera kulandira mpeni podula uchimo. Tiyenera kuthandizana pochita zimenezi kwa ife ndi mpingo, zimenezi ndi zeni-zeni zoonza Mulungu anti “Yesani, ine yesani ine muona” kumvera njira ya Yesu ndi kukhala ansembe tsiku ndi tsiku. Khalani ansembe pa okuzungulilani pelekani matupi anu monga nsembe ya moyo ndi kuthandiza ena kukhala ngati Yesu ndipo Mulungu adzathira madalitso mu mtima mwanu.

Bwelani Mudzapeleke

Pali mbali ina imene pokhala wansembe uyenera kuidziwa. Iyi ndi yochepa polingana ndi zina zimene talankhula kale. Muyenera kupeleka nokha monga nsembe ya moyo ndi kubweletsa Yesu kwa anthu, kuwathandiza iwo kukhala monga Yesu analiri. Koma plai mbali ina pokhala wansembe imene imakhudza pa msonkhano kapena pokumana. Ngati simunapeleke matupi anu monga nsembe yamoyo pokonda anthu mu malo amene mukhala, ndi kuthandiza ena kukhala ofanana naye Yesu mu moyo wa tsiku ndi tsiku ndiye kuti msonkhano ulibe kanthu koma ngati mukuchita zimenezi pokhala wansembe ukunso ndi mbali yokhala wa nsembe.

Ngati Yesu adakakhala muthupi mu chipinda chino nthawi yino. Akonza kukhala phee nthawi zina koma nthawi zina Yesu amakhala ndi zofunika kulankhula. Yesu ali pompano ngati mukhulupirira kuti muli ansembe chifukwa Mulungu adatero mu mwazi wa Yesu (osati mukumva motero, nzeru kapena mphamvu) ndiye muyenera kukhala wa nsembe pa nthawi imene woyera ali pamodzinsu. Ngati Yesu akhala mwa inu ndipo munabatizidwa mwa iye mu moyo ndi mzimu wake, pameneponso mungamvenso Mulungu. Monga wansembe, mudzabwera kupeleka. Bukhu la Ahebri limalankhula za izi

“Ndipo tiganizire wina ndi mzake kuti tifulumizane ku chikondano ndi ntchito zabwino osaleka kusonkhana kwanthu pamodzi monga amachita ena komatu tidandaulirane, ndiko koposa monga momwe muona tsiku lilikuyanduka.”
Ahebri 10:24–25.

Taganizirani kufunika kwa kukondana ndi ntchito yabwino choncho mong wa nsembe ndi mabwera pakati pa abale ndi kuona mene tingaperekere, ndingaperekere motaninsu. Muyenera kukhala olimbika mtima Kunene zimene Yesu afuna. Osaopa kulakwitsa ngati mwalakwitsa mudzakula ndiye motero kofunika kukhala nonse pamodzi mujsakhale anthu osafunana khalani nonse nthawi yonse pamene muyembekezera kudza patsiku la Ambuye, Monga Yesu adza posachedwa.

Osazimbaitsa, Mwamva

Yesu anakwiya, anakwiya pa zinthu zochepa. Yesu anakwiya kwa onyenga. Anakwiya kw anthu amene amayekeza kukhala njira ina pamene mu mtima muli kusiyana njira. Yesu anakwiya pa zimenezo ndipo ali choncho mpaka lero. Tisanyenge kuti tili otere pamene sichoncho. Pamene zoonza mu moyo tili mu njira yosiyana. Tiyenera kulankhula za izi ndi abale athu ndi kufuna kuthetsa mabvuto poyera ndi moonza. Mulungu anati “*muulure uchimo kwa wina ndi mzake*” kuulura ndi kupemphera kuti tichilitsidwe. Anthu ambiri ali odwala mkati muuzimu kapena mthupi chifukwa satsegula mitima yawo ndi kunena machimo awo kwa anzawo, amaopa kuchita chomwechi. Koma mu nyumba ya Mulungu tisamaope ali chifukwa timakondana wina ndi mzake ndipo tifuna kuthandiza. Sitichita miseche sitidzakanana. Tidzathandizana wina ndi mzake, choncho tingawulure machimo athu mwaufulu. Tidzamva chisoni koma osaopa konse. Yesu adzathandiza ife ndikutitchuka ife koma ngati tinama kuti tilibe uchimo, ndiye tili achinyengo ndipo Yesu amakwiya. Yesu anakwiya, amakwiya ngati tili achinyengo sitifuna Yesu akwiye chifukw acha ife. Timachita ife? Choncho titsegule mitima yathu.

Musakwirire Luntha lanu

Yesu anakwiyanso ndi munthu wina, anakwiya kwa munthu amene anakwirira luntha lake. Ndipo Yesu anamutcha munthuyo wantchito oipa. Anamutulutsa kunja ku mdima. Chimene ndili kulankhula nanu ndi ichi, monga wansembe simuyenera kubisa luntha lanu. Mulungu anapeleka kwa wina aliyense wa inu china chake chapatali pa moyo wake. Ngati muli wa nsembe, gwilitsani ntchito chimene Mulungu anakupatsani. Munthu uyu mu fanizo limene anakwirira ndalama ali wamantha.

Yesu sanakondwere naye ai pokwirira luntha lake. Pamene oyera mtima ali pamodzi Yesu safuna kuti mungokhala, kumvetsera ai. Safuna kuti inu mukwirire chimene anaika mwa inu inu ndinu ansembe. Limbikani, mphamvu ndi chikhulupiriro mwa Mulungu kuti mungakwanitse kulankhula mu mphatso imene anakupatsani inu, aliyense wa inu ndipo musaope monga munthu uyu mu fanizo.

Lingalirani monga mmene mungachitire ndi ena ngati muli wansembe pamodzindianthuozunguliranandiokhulupirandithupilanuchoncho mungathe kukhala wansembe pamene abale ali pamodzi. Muyenera kufuna kubweletsa nyimbo imene ili pamtima wanu. Aphunzitseni anzanu nyimbo imene mwaphunzira pamene mumapephera ndi Yesu m'mawa, kapena muzawelenga limodzi la Masalimo ndipo mudzafunsa Yesu kuti akupatseni mang'ombe abwino pa nyimboyo. Ndiye monga wa nsembe bwelani ndi kubweletsa woyera mtima pamodzi, ndi kuphunzitsa nyimbo imene Yesu wapeleka kwa inu. Ndiye wa nsembe muyenera kutero ngati wansembe musakwirire luntha lanu.

Mwina mbale adzabwera nalankhula za uchimo mu moyo wanu. Mumveleni iye ndipo zibweletsa misonzi mu maso mwanu. Monga nthawi imene Natani adalankhula kwa Devedi ndipo Devedi anasweka mtima, Mulungu anatuma Natani – mbale kwa inu ndipo adzanena zauchimo ndipo uzaswa mtima wanu. Mudzalankhula ndi Yesu paizi ndipo ndi kulingalira malembo ena pa izi. Kenaka mudzabweletsa abale pamodzi pa malo amodzi ndi kuwauza m'mene Yesu waphunzitsira inu. Auzeni malemba amene mwawaphunzira amene asintha moyo wanu. Auzeni m'mene munagwera ndi m'mene iwo sangagwelenso. Awonetseni zinthu zimene Mulungu waonetsa kwa inu. Ameneyo ndiye wansembe. Inu ndinu ansembe mungatenge zinthu zimene Mulungu wachita mwa inu ndi kutsegula kwa abale ndi alongo. Mulungu akufuna kuti tidzitero tonse amene. Muli wolora kutero?

Choncho tabwera pamodzi mudzina la Yesu ndikumvetsera. Koma Yesu sakhala chete kwa nthawi ngati zinthu zili chete kwa nthawi yaitali chifukwa ndi choti wina siwansembe wabwino, kapena ndikumvetsera. Koma Yesu sakhala chete kwa nthawi ngati zinthu zili chete kwa nthawi yaitali chifukwa ndi choti wina siwansembe wabwino, kapena Yesu afuna kuti inu mugawe nyimbo ndipo mukuopa. Kapenanso Yesu akufuna

kuwelenga malembo amene anali apamtima wanga m'mawa uno, koma ndimaganiza Ai, sindili wabwino konse sindingathe kutero. Kenaka zii, chifukwa Yesu amafuna kugwiritsa ntchito ine koma sindinamulore ndifuna kuti ndikwilire luntha langa ngati Yesu anakakhala pano mu thupi, sanakakhala chete kwa nthawi yaitali chifukwa pali zambiri zimene Yesu amafuna kuti zichitike m'moyo mwathu. Ngati ife tili ansembeabwino, tidzamvera Yesu. Yesu adzagwiritsa ntchito aliyense wa ife. Adzakhala mwa ife kubyalera mw ansembe ake, ngati tili ofuna, muli ofuna kutero? Landilani Yesu agwiritse inu ntchito.

Akufuna kuchita zodabwitsa

Kumbukirani kuti Yesu pamene anapita ku malo ena anafuna kuchita mirakulu kumeneko, koma sanachite chifukwa anthu anali osakhulupira. Muyenera inu kukhulupira mu mtima mwanu kuti Mulungu afuna kukugwiritsirani ntchito. Muyenera kulankhula ndi Yesu pa zinthu izi. Muuzeni iye: Ndimakhulupilira ndithandizeni “kusakhulupirira” funsani iye kuti mukhale ofewa ndi ozichepesa. Funsani Yesu kuti akuthandizeni kuti mulimbike kuona mphatso yanu, funsani Yesu kuchotsa kunyada, chifukwa nthawi zina mudzakhala olakwa. Koma ndizabwino kulakwa ndipo tonse tingathandizane. Ndibwino kulakwa kusiyana ndi kukwirita luso lanu. Ngati mwalakwatsa tikhonza kukhala tonse pamodzi, koma ngati mungakwirire luso lanu. Yesu ali okwiya, ndiye funsani Yesu kuti akuthandizeni inu kuti mukhale wansembe wabwino.

Izi sizofunika kuganiza mozama kapena kulankhura bwino. Izi ndi kufunsa Yesu kuti athandize inu. Iye ndi wamoyo, akufuna kugwira ntchito yodabwitsa mu mitima kuphyola mu mitima ya ena. Koma kwa iye kuti achite mirakuli, tiyenera kukhulupilira, ndiye lankhulani ndi Yesu za zimenezi. Mwangoganiza chabe mu mutu wanu ndi kubvomeleza izo chabe. Malomwake, lankhulani ndi Yesu wa moyo pa zinthu izi ndipo adzatithandiza ife tonse, ku ulemerero wake.

Afunseni kuti akhale Ansembe

Pamene muli ansembe kwa abale anu mungathenso kuwathandiza kuphunzira kudziwa Yesu ngati ali kumbali ya chipembedzo kwina kake,

apempheni kuti akhale ansembe kumene akhalako, Apempheni kugwilitsa mphatso kwa anthu amene azungulira. Asangopita ku misonkhano kwawo kukamvera chabe. Funsani iwo kuti ayang'ane kuti ayang'anire miyoyo ya zongulira iwo ndikuwathandiza kuti akhale monga Yesu. Ngati wina kulikonse achita izi. dziko lizasinthika. Zimenezi ndi zamphamvu – chifukwa ndalora kuti Yesu akhale Yesu. Ngati sindingathe ansembe Yesu amakhala mu botolo kapena mu Bukhu, ngati tili ansembe ndi kufunsa wina aliyense amene abvala Yesu kukhala wa nsembe. Yesu adzaloledwa kuti akhale Yesu PALIPONSE! Midzi yathu idzasinthika mizinda yathu idzasinthika. Maiko ndi maiko akulu onse adzasinthika ndipo Yesu adzakhala Yesu ngati ndidzakhala ansembe! Amen?

Pamene tinadziwa Yesu zaka khumi zapitazo, taphunzira mopitilira mmene mpingo uli ndi wansembe alili, ndi mmene tingakhalire wansembe. Pamene taphunzira zinthu izi zinatitengera ife kumachitidwe odziwa kuchita ndi chipembedzo. Anthu a chipembedzo si adani athu. Ambiri ali kumeneko chifukwa ndi zimene iwo adazidziwa. Ngati atidziwa Yesu kwambiri adzakondwa kumutsata. Ndiye ndi chofunika kuti tikonde anthu ngakhale a muchipembedzo. Ife tili osamalitsa kuti tisanyade. Pamene Mulungu akupatsa ife opempha monga ife chakudya cha nyenyekwa. Tiyenera kugawa chakudya ndipo osaweluzana ena pokhala alibe chakudya. Iyi ndi njira ya Yesu kugawa chakudya chimene wapeleka kw aife – osati tigawikane chifukwa cha chakudya, koma kupeleka chakudya.

Zinthu izi ndi zofunika kwambiri kukhala mu mitima ndi mmaganizo. Sitidzalora kutentha chabe kapena kunyengalera. Koma timakhulupirira Yesu adzamanga mpingo wake, ndiye pamene tipeza anthu amene akonda Yesu mu zipemphedzo, kapena tisati chaokani, chokani mmalo mwake “mvelani Yesu ndi anthu amene muwadziwa “Timawaphunzitsa njira ya Yesu monga mmene anatiphunzitsira ife. Timawafunsa kuti aphunzitse aliyense amene amudziwa njira ya Yesu. Ngati achita motere mu mipingo adzathamangitsidwa mu chipembedzo anthu ambiri samvera Mulungu ena amamvera, komanso ena ai.

Mu mpingo wona umene Yesu akumanga, ALIYENSE amafuna

kumvera Mulungu ndipo ALIYENSE amakonda Yesu. Chifukwa tonse tili ansembe ndipo timathandizana wina ndi mzake ngati wina sakonda Yesu amathawa.

Mu uneneri mu Yereimiya 31 wa mpingo wa chipangano chatsopano ndi oti, *“onse adzandidziwa ine kuyambira aong'ono mpakana akulu”* mu mpingo wona onse amadziwa Yesu. Mu chipembedzo chimene sichoona ndi mmene muli kutentha chabe.

Anthu amakonda dziko ndipo amakhala mu uchimo ndipo sasintha. Ndi zoipaizindizobvutakwambiri. Komaplainso anthu abwinomu chipembetso . ntchito yathu sikuti anthu achokeko. Ntchito yathu ndi kuthandiza iwo kukhala ansembe kumalo amene iwo ali. Ngati adzakhala ansembe pamalo amene ali anthu ambiri adzasinthika kapena atachotsedwa.

Pamene Yesu ali ----- chimo silingakhale

Ngati mbale kapena mlongo afana ndi Yesu ku chipembedzo, kapena chipembedzocho chidzasinthika, kapena chidzawapha kapena kuwataya (monga momwe adachitira ndi Yesu) sitikuopa zipembedzo. Ali ngati khoka lalikulu limene lisunga nsomba zosiyana siyana. Pali nsomba zina za bwino mu khoka ndipo zina nsomba zoipa. Ntchito yathu ngati ansembe ndi kuitana nsomba zonse zabwino kuti zikhale ansembe kumene iwo akhalako.

Kodi Neneveh anasintha? Yona analabvulidwa ku kamwa kw ansomba nalowa mu mzinda oipa uja. Uchimo umalipo kumeneko koma mzinda onse anasintha kwa Mulungu ngakhale mfumu. Tiyenera kukhulupirira Mulungu kuti angapange mu chipembedzo. Tikhulupilire kuti angachite izi ku Mzuzu, ndiye ngati tili ndi abwezi kapena anthu amene timadziwa mu chipembedzo, sitimauza kuti achoke, timawauza kuti akhale ngati Yesu ndi mtima wawo yonse kulankhula mau a Mulungu kwa aliyense amene amuone kumeneko, kutaya moyo wawo, kukonda anthu osanyengelera kapena kuopa kunyengeledwa. Anthu a ku Neneve nasinthika ndi moyo wathu ku chipembedzo kumene tikhale ansembe ndi kuyesa kusinthika. Tidzayensa kuthandiza anthu abwino amene timawadziwa ku chipembedzo ndi kuwafunsa kuti akhale ansembe kume ali kuthandiza anthu owazungulira kusinthika.

Timupempha Mulungu ndi misonzi yambiri kuti chipembedzo chisinthe Yesu analira. Anathets amisonzi ndi Yerusalemu. *Anati ndinakakusunga iwe monga mmene nkukhuku imasungira anapiye ake.* Koma Yerusalemu sanafune ndipo anamkana iye – Anamupha. Ngati tili ansembe okhulupilika, adzatipha kapena mzinda wonse udzasintha. Koma tiyenera kukhala ansembe okhulupilika. Tiyenera kufunsa ansembe amene timawadziwa kuti akhale okhulupirika ku malo amene akhala. Ngati adzayese kuthandiza anthu amene amawadziwa, adzakhala olimba kapena kuchotsedwa koma ndiye kuti akhonza kukhala ndi okhulupirira ena amene ali ndi moyo umodzi, titayensa ndi anthu otizungulira ife. Ndizimene wansembe amachita. Tiyenera kukonda amene ali mu chipembedzo. Ndi zimene Yesu anachita. Koma tisalore kunyengedwa. Tiyenera kukhala mu choonadi ndi kufuna mu choonadicho. Ngati aliyense adzatero, pamenepo Yesu adzamanga mpingo wake.

Uwu ndi uthenga wabwino wa Yesu. Tiyenera kukhala njira yotere kwa anthu okhala nawo. Osanyengelera osakhala ozizira--- *koma tiyenera kuwakonda ndi kuthandiza iwo.* Pasakhale kusiyana kukhale chifukwa wina safuna kumvera Yesu. Sitidziwa izi mpaka titayesa. Umu ndi mmene tingakhalire ndi chipembedzo. Tiyenera kutaya moyo wathu kwa iwo ndi kuchita chilichonse chimene tingapeleke mkate wa moyo ndi kufunsa iwo kuchita ndi anthu amene amawadziwa ndiye tiona ndi kuyang'anira chimene Yesuachite ndi chimenecho. Yesu anati ngati tidzachita mbali yathu. Iye adzamanga mpingo wake ndi makomo a ndende ya mtima sidzaima. Tikhononga mzinda wa Satana kuphwasula ndi kuwononga makomo onse. Timakonda anthu ndi kuwabweletsa kuchokera ku Mtima ndi ku kuwala. Sitikusiyana pa maina koma tikonda anthu – mphaka ku imfa. Timachita ntchito yawa nsembe ndipo Ambuye adzamanga mpingo wake.

Yesu Yekha Ndiye Bwana

Mlowe, Africa 1996

Chimene chipanga Mtsogoleri?

Pali mitundu iwiri ya atsogoleri, wina ndi mtsogoleri ochokera mu mtima, kuchokera mu mulumikizo ndi Mulungu wina ndi mtsogoleri wa undindo ndi mpando ndi olemekazeka “wamkulu” Bwana olemekazeka, Yesu anati mtsogoleri utero asakhalepo. Atsogoleri a mpingo ndi amene akuyenda ndi pafupi ndi Mulungu LERO ngati mbale kapena mlongo sakuyenda pafupi ndi Mulungu lero, sayenera kuganziridwa kukhala mtsogoleri. Ngati munthu sabata yatha samayenda ndi Mulungu koma walapa pa machimo a mu moyo ndipo akumva Mulungu, ndipo ali mtsogoleri lero koposa sabata yatha. Kukhala mtsogoleri zimachokera ubale ndi Mulungu ndi anthu a Mulungu sizichokera pa ofesi kapena undindo.¹

Tili ndi atsogoleri kumene ine ndimakhala, koma kulibe “maofesara” mtsogoleri lero koma sabata in ai. Yesu anati ulamuliro yonse m'mwamba ndi pansu pano uli PAINE. Zimenezi ndi zoono, choncho, m'mene tingamvere Yesu, amene ali ndi, amene ali ndi ulamuliro. Ndi m'menense ali ndi ulamuliro nawo – pamene akwanitsa kumva Yesu, ndi choncho. Ulamuliro wonse “kumwamba ndi pansu pano” uli pa Yesu. Iye anati munthu amene sadziwa Yesu angakhale ngati choyelekeza chabe. Munthu ameneyu amafuna adziopedwa pamene afuna zitero, ngati ali ndi mpando koma ali mtsogoleri ngati amadziwa, kukonda, ndi kumvera mutu Yesu.

Kubadwa kuchokera mu Ulesi

Pali mayambidwe ochokera mu ulesi mwa ife zimene zimapangitsa ife kubisala pansu pa nthaka ndi kulora wina atimenyere nkondo ndi zimene akulu ndi opanda undindo zinayambira. Poyambilira pomwe mu mbiri ya mpingo kumbuyo ndithu zaka zikwi ziwiri zapitazo zaka 1800 zapitazo anthu anayamba kufuna mfumu kuti adzawalamulira. Anafuna kuti “munthu oyera” akhala mtsogoleri wa mpingo.

Mwina munthuyo analidi pafupi ndi Mulungu koma mmalo mufuna kuti aliyense akhale wansembe. Anthu a Mulungu anafuna kukhala ndi munthu mmodzi woyera kuti adzimenyera nkondo. Anafuna kutenga munthu mmodzi ndi kumuika kukhala “mfumu wa mpingo”

Munthuyo mwina anali wabwino. Bvuto siloti munthuyu anali pa ubwenzi ndi Mulungu. Mwina munthuyu anali ndi mphamvu ndi mphatso, koma pamene ayikidwa padela monga ya padera ndikutchedwa “bwana wa mpingo” Pamanepo pali bvuto malo amenewo ndi a Yesu yekha Yesu ndi bwana wa mpingo wona. “Abusa sayenera kukhala bwana wa mpingo palibe mabwana koma Yesu.

Pali chitsanzo m’Baibulo cha mautsogoleri awiri amenewa. Samueli ndi Sauli onse adali atsogoleri a anthu a Mulungu, Israeli. Samueli adali munthu wa Mulungu amene adali ndi chikoka mu fuko chifukwa amadziwa Mulungu. Samueli adali ndi zothekera zambiri zaufumu ku Israeli—koma Samueli sadali mfumu! Komabe, Sauli adatchedwa mfumu. Israeli imafuna kukhala ndi mfumu—amafuna kukhala ndi munthu modzi kukhala bwana. Amafuna wina kuti alowe mmalo mwa Samueli ndipo amafuna “mfumu” monga mafuko onse owazungulira. Munjira ina utsogoleriwo ukhonza kuwoneka mofanafana, koma Samueli alibe “mpando” wa ulamuliro. Samueli amagwira ntchito kuchokera paubale wake ndi Mulungu, ndipo Sauli amagwira ntchito kuchokera pampando wake. Samueli adalibe ofesi, mlembi kapena malipiro (salare). Iye sadali muudindo wa mpando ngati mfumu. Samueli adali chabe munthu wa Mulungu amene amalemekezedwa ngati mfumu koma adalibe mpando kapena ofesi. Iye sadali mfumu iye sadali “mbusa”. Iye amangokonda Mulungu ndi mtima wake onse.

Ndipo chifukwa choti amamvera Mulungu, adali ndi chikoka. Adalibe mpando adali ndi chikoka. Ngati munthu moonadi adziwa Mulungu, adzathandiza anthu a Mulungu. Ngati wayitanidwa ndi Mulungu, adzakhala akuthandizila anthu. Ndibwerezanso: Munthu wa Mulungu oona alibe mpando... ali ndi chikoka. Yobtu 29, ikulongosola za munthu olemkezedwa ndi Mulungu ndi anthu, ndi woopedwa ndi odedwa ndi satana. Munthu otere safuna ofesi kapena dzina kapena malipiro. Ngati muli ngati Yesu, simudzafuna “mphamvu.”

Mongamwachitsanzo, ngatindilim’ misili, ndi mapangazinthu dimatabwa. Ndimapanga mpando, tebulo kapena chitseko kuchokera ku matabwa. Ngati ndili omanga, ndiye kuti ndimanga zinthu ndi njerwa. Chinachake chomwe ndipanga kuchokera ku njerwa ndi umboni oti ndine omanga. China chake dzomwe ndipanga kuchokera kuthabwa ndi umboni oti ndine m’ misili. Tsopano, mu Baibulo mau awa “mbusa” (kutathauza kolakwika) koma atanthauzira kuti mphatso ya ubusa wa nkhosa, ogwira ntchito tsiku ndi tsiku pakati pa anthu a Mulungu moyendezana (mwapambali) pa mphatso zina—osati bwana kapena “olankhula wamkulu” pamsonkhano. Kodi umboni uli pati kuti ndine Mbusa weniweni? Umboni ndi wakuti ine ndimakonda anthu a Mulungu! Ndimawathandiza iwo usana ndi utsiku. Sindifuna dzina, sindifuna kukhala bwana. Ndimangokonda anthu ndi mphatso yomwe ndili nayoyi, ndikuwathandiza. Umboni waumusili ndi mpando omwe ndapanga umboni woti ndine Mbusa weniweni ndi woti ndimadyetsa anthu a Mulungu tsiku ndi tsiku, ndipo ali chifupi ndi Yesu chifukwa cha ine. Ngati ndiwona kuti m’modzi mwa anthu a Mulungu ali ndi njala, chimandiswa mtima. Ngati ndiwona kuti m’modzi mwa anthu a Mulungu ali muvuto kapena muzoopsa, mtima waubusa mkati mwanga uthamangira iwo kukawateteza. Uwu ndiye umboni oti ndine odzodzedwa wa Mulungu kukhala m’busa. Sindifuna mayina opatsidwa. Sindifuna chitupa chopachika pakhomo ndi chochokera ku Sukulu ya Baibulo. Ndifunitisa mtima okonda ndi kuchita ntchito ya Mulungu, ndipo kenako ndizabala zipatso zauzimu mumbali iliyonse yomwe iye azandipatsa ine.

Tsono, ndinu m’ misili? Ndiye pangani mpando. Muli ndi mphatso ya ubusa. Ndiye kondani anthu—adyetseni, atetezeni ndipo athandizeni. Ichi ndi choona pa mphatso iliyonse! Umboni wa mphatso iliyonse uli mudzipatso zimene umabereka.

Zotsutsana za zonsezi ndi zoonanso ndithu. Ndifundo yodabwitsa kuti amafano mu sayansi ndi mankhwala ndi malonda amalamula kuti amene ali ndi maganizo ndi mtsutso ndi odzitcha okha “akatswiri” ali ndi china choti awonetse, zipatso mumiyoyo yawo, awonekera kuti ali dni ufulu wolamulira, kuphunzitsa kapena kutsutsa ena. Mudziko lachipembedzo, modabwitsa, ali ndi ungiro ochepa kuposa ngakhale zimene amafano amaonetsera. Muchipembedzo, ngakhale, anthu ali akhungu ndi wozunguzidwa kwambiri.

Mtsutso, ukatswiri, zigamulo, ndi ngakhale ubale ndi zonyoza zimayenda mophweka kuchokera kwa iwo azipatso zoyipa miyoyo yawo, m'mabanja ndi m'mabwalo awo. Zodabwitsa, koma zoonu ngati inu muona chipembedzo chamunthu mosamalitsa ndi moonu. Munthu amene amapanga zinthu zotere ngati bodza kapena m'nyozo kapena kukhala ngati katswiri pa njiniring'I, zamakhwala kapena malonda akhonza kusonkhanitsa pamodzi gulu lomvera mpphweka anthu akuopa, m'mene akhonza kunderedwa pansu, kapena kuyamikiridwa mpusitsa ku—kuzipereka ku makina osabereka zipatso ndi “akatswiri” zonga zamisala koma ndi zoonu. Zimachitika kunthawi zonse, chifukwa umu ndi m'mene maufumu a vuto amasungira nambala yao. Mantha ndi kuyimikira kopusitsa, mjedo, m'nyozo kapena kuyenderedwa pansu. Nchifukwa chake ziri zosadabwitsa kuti Yesu sanapange bwino mu chipembedzo chovomerezedwa kudziko lapansi cha munthawi yake. Koma, likhonza kuphunzira kwa iye ndi kusunga malembo, ndi kuyang'ana zipatso, osati kumvera—kunena kwa mfundo ndi mabanjeti, ndiponso kunena kufuna kwa yenkha kwa munthu kuti ateteze.

Pamenepo mwatengapo mfundo.:

“Mwandikana ine”!

Izi ndi zoonu kwa mphantho iliyonse koma anthu aononga kwambiri chi Kristo pofuna kukhala ndi mfumu Samuel sanali mfumu, anali munthu wa Mulungu. Sauli anali mfumu ndipo anaononga anthu a Mulungu. Mulungu anati “sanakukane iwe, Samuel, Akana Mulungu. Samueli anali wa chikoka chifukwa amadziwa Mulungu, sichifukwa choti anali pa udindo wa Ufumu.

Ndipo iwo anatengera, sanatengere? Wina wochokera dziko lina amanena akafika ku Israel, muli ndi mfumu! ‘Samueli ndi mfumu yanu’! A Israel amati “inde” tikudziwa akuoneka ngati mfumu, chifukwa ali otamandika ndi opatsidwa ulemu koma Sali mfumu. Tilibe mfumu ife, tilibe mfumu koma Mulungu. Samueli amadziwa Mulungu bwino, ndiye tikupatsa ulemu ndi kumukonda. Maiko ena maganiza kuti a Israel anali ndi mfumu, mfumu Samueli koma sanali mfumu anali munthu wa Mulungu. Analibe mpando. Mapita pano ndi uko kenako osaonekansa, ndi kubwelanso.

Maufumu sapangaz zimenezo. Amuna a Mulungu amatero. A Israeli anafuna kuika wina mmalo mwa Samuel pamene anakalamba anafuna kukhala ndi Mfumu monga maiko ena onse (kapena monga zipembedzo zina).

Pamene tifuna munthu wina kukhala bwana wa ife kuti atimenyere nkondo, ndiye takana Mulungu 1 Samueli 18:7 “*sanakane iwe, Samueli, andikana ine*” tisayese kukhala ndi anthu okhala bwana. Tiyenera kuwakonda ma Samuel pakati pathu amene adziwa Mulungu, talemekeze ndi kuwamvera, pamene sakukhala ndi udindo kapena bwana kupatula Yesu yekha basi, timvere Yesu, kulankhula mwa Samueli, Lolani Samueli woyamba akhale pansu. Izi ndi zabwino.

Zotsatira zake

Ndikufuna kuti mumve zimene inu ngati mukhala ndi mfumu. Pamene mufuna kukhala ndi “Bwana wanu” Bwana wa mpingo. Izi ndi chipatso zochokera mwa izo

“Nati, Awa ndi makhalidwe a mfumu imene idzaweluzidzatenga ana anu amuna, akhale akusunga magaleta ndi akavalo ake ndipo adzathamanga ndi kutsogolera magaleta ake adzawaika akhale atsogoleri zikwi ndi atsogoleri makumi asanu ndipo adzaika ena ndi kulima minda ndi kutema zinthu zake ndi kumpangira zipangizo za nkondo, ndi zipangizo za magareta ndipo adzatenga ana anu akanzi apange zonunkhira naphikire naumbe mikate ndipo adzalanda minda yanu ndi minda ya mphesa yanu ndi minda ya azitona inde minda yoposayo, nadzaipatsa anyamata ake ndipo adzatenga limodzi la mayawo khumi la mbeu zanu ndi minda yanu ya mphesa nazaipatsa akapitawo ake ndi anyamata ake. Ndipo adzatenga akaporo, ndi azakazi anu ndi anyamata anu okongola koposa ndi abale anu nidzagwiritsa ntchito zake. Idzatenga limodzi la magawo khumi la zoweta zanu ndipo inu mudzakhala akaporo ake, ndipo tsiku lija mudzafuula chifukwa cha mfumu yanu munadzisankhira nokha, koma Yehova sadzayankha inu tsiku lijalo. Koma anthu anakana kumvera mau a Samueli nati Iai, koma tikufuna kukhala nayo mfumu yathu kuti ifenso tikafanane nao anthu a mitundu yonse kuti mfumu yathuyo ikatiweluzire ndi kutuluka kutitsogolera ndi kuponya nafe nkondo zathu. (1 Samueli 8:11 –20)

Pamene tifuna mfumu atilamulire, pamene tifuna olemekeseka bwana mu mpingo, iye adzaba masomphenya adzaba ana athu ndi ndalama

zathu ndipo tidzakhala ife otigwilitsa ntchito chabe. Zinthu izi sizabwino koma zikuchitika mu dziko lonse la chipembedzo. Kumaiko ena onse amene tapitako pamene pali bwana ndi munthu wamba, pamene pali anthu osiyana akristo. Bwana ndi munthu wamba – mitima ya anthu ndi mphatso sizimagwira ntchito. Mphatso ya chifundo ndi mphatso ya kuthandiza imachotsedwa pamene munthu mmodzi ali mtsogoleri otere osati Yesu kukhala bwana, mitima ya anthu imabedwa.

Anthu a Mulungu anali opeza bwino mu ulamuliro wa Samuel iye sanali ndi udindo, anali ndi mphatso zinali ngati zophweka kusintha kuchoka kwa Samueli kupita kwa Sauli chifukwa amaoneka ngati onse ndi mfumu. Koma ina inali mphatso ndi ina udindo, pamene pali mphatso, Anthu a Mulungu amalemera. Pamene pali udindo olamulira anthu, anthu a Mulungu amabvutika, molingana ndi mau a Mulungu. Mulungu angagwiritsidwe ntchito pa zabwino zokha. Devedi anali mfumu yabwino. Zinthu zina zabwino zingaoneke ngakhale kuti njira ndi yoipa. Koma Mulungu anati “Ndili nayo njira yabwino” njirawo ndi Samueli, osati Sauli, iye anati, Ndingachite zinthu zina zabwino ngati mukhala ndi mfumu, koma pamene mabvuto abwera mudzalira kwa ine ndipo ine sindidzayankha” Izi ndi zimene zikuchitika mu chipembedzo, chifukwa amamanga pa mphatso ya munthu kukhala mfumu. Sauli ndipo analoledwa kumuika kukhala mfumu.

Zinthu zina zabwino zikhonza kuchitika koma mu tsiku la zowawa adzalira kwa Mulungu ndipo sadzamvera iwo, ndipo zinthu zidzatakilana. Padzakhala ndale ndi mphamvu kuchitidwa ndipo padzakhala miseche ndi zamwano ndipo matemberero onse adzakhala amene Mulungu anawanena. Pamene Mulungu angathe kuchita zinthu zambiri mu zochita zilizonse. Timafuna zabwino zokha. Sizabwino zimenezi? Mulungu angadalitse chilichonse mu chifundo chabe kukoma mtima ndi kupilira. Koma tiyeni timange kuti tilandire madalitso ambiri! Tikhale ndi ma Samueli pakati pathu mmalo mwa Sauli m’modzi. AMEN?

Chinanso chimene chachitika ndi choti munthu kupita ku seminare kukatenga chizindikiro cha chipemphetso, angakhale kuti mtima ungakhale wabwino amakakamizidwa ndi udindo kukhala zimene iye saali. Angakhale ndi mabvuto nyumba mwake, ndi ukwati ndi ana ake ndi ogona nawo limodzi ndi makolo mwachoncho, chifukwa ali ndi udindo

wa chipembedzo anthu amayankhana kwa iye, mmalo mokhala mbale pakati pa abale. Amachita zinthu zina munjira ina kusiyana ndi mmene amachitira kunyumba, monga kuyenera kukhala mbale pakati pa abale. Pali zina zimene zili mkato mwa ife zimene zimapangitsa ife kusafunsa moyo wa Bwana. Pamenepo atsogoleri mu mpingo asafune maudindo zimene zingaimitse zinthu zothandiza ena mu moyo wawo.

1. Mau oti ofesi amathandauza ngati ndi olemekezeka” okhalapo chilichose chokhalapo pa anthu a Mulungu kaya mu nyumba kapena munthu odziwika.

Devedi Living'isitoni Ndi Mkate Ochokera Kumwamba

Chilembe, Africa 1996

Mkate wa Moyo

Mbale analankhula za Devedi Livingstoni kubweletsa mkate ku Afrika. Devedi anabweletsa ku afrika chiphunzitso cha Yesu mwana wa Mulungu. Anabweletsa uthenga mmene Yesu amakondera anthu, amafunira kukhulukira machimo athu onse ndi kubweletsa moyo wa tsopano. Tikudziwa kuti uwu ndi uthenga wabwino kwa ife. Devedi anabweletsa mkate m'mbale ndi chobvundikira, ndipo ndamva mmene mkatewo unali kukoma.

Timabwera tonse la Mulungu ndi kulankhula za mmene mkate unaliri ndi chiphunzitso choona. Mkate ndi wabwino ndithu mbali ya uthenga umene Mulungu watiitanilako ife sikungophunzitsa mmene mkate, koma zimene Baibulo amati “mafungulo a mu ufumu” ziphunzitso za Yesu mmene tingatsegulire khomo ndi ziphunzitso mmene tingachotsere chovindikira ndi kutilora ife kudya mkate umenewu.

Yesu sanangatikhulukira machimo monga zodabwitsa monga ziliri kapena kuti tiganize za chiphunzitso chake. Yesu anabwera kuti ife tikhale ndi moyo umene iye anakhalira ndi Atate – osati kudzakhala chabe, kufa ndi kupita kumwamba. Monga Baibulo linena. Anabwera kuno kuti tikhale mu “mphamvu ya moyo wagwiro” kukhala mu chiyanjano ndi moyo ndi chikondi pamodzi ndi atate ndi abale amene Yesu anachita.

Yesu amafuna ife kukhala kuthyola ziphunzitso za mkate mu mphaka, akufuna ife tidye mkate umene iye anadya ndi Atate ake.

Mkate Umodzi

Zambiri zimene chipembedzo ndi chikristo chachita kwa zaka zambiri ndikutiphunzitsa mozama za mkate. Ndi nthawi yoti tidye mkate ndi

nthawi tsopano tichoke kuchokera kuphunzira ziphunzitso za mpingo ndi kukhala mpingo (Aefeso 3:10, Mateyu 16:18) Yesu sanabwere kuti tikhala ongooneka bwino. Anabwela kudzatipatsa ife moyo ochuluka – tikhale mu moyo wake tsiku lililonse wina ndi mnzake, osati kulankhula mau wake obweleka ndi kuyimba ndi kupemphera mau a chipembedzo. Anabwera kudzatipasa MOYO! “Ana ang’ono, kondani ndi mzake” uwu unali chiphunzitso cha Mulungu mutu ndi Yesu NDI Yohane ndi Paulo ndi Petro.

Timaphunzitsa za banja la Mulungu, osati chipembedzo chokaonera. Kodi ife timaonera zochitika m’banja lathu? Kapena tikhala mchikondi ndi mabanja tsiku lonse? Simungaonelere banja mukhonza kukhala banja. Baibulo limalankhula bwino za izi. simungaonelere chipembedzo choona, mukhonza kukhala mpingo woota. Banja limene mungaonere ndi losunga ana amasiye osati banja lowona. Kusunga ana amasiye kumakhala bwana wake ndipo amasonkhana onse kudzadya chakudya. Mwina amapita ndi kusewera pamodzi ndi kulandira chiphunzitso kuchokera kwa mabwana awo. Choncho limachita zambiri zimene banja limachita, koma ndi ana amasiye osati banja. Mulungu waitana ife kukhala banja tsopano ngati simuli banja, padzakhala kusintha kumene kudzakhala popeza Yesu. Pofuna kudziwa Yesu ndi kudya mkate, tiyenera kukhala mkate ndipo ngati tingakhale banja la Yesu, tiyenera kuthandizana zedi. Sitiyenera kukhala wozikonda. Tiyenera kusiya kunyada ndi kufuna kutsegula kwa anzathu za Yesu kusintha moyo wathu.

Tiyenera kukhala okhulupirika wina ndi mzake zamene tikumvera. Sitiyenera kubisa kumbuyo ka nkhope kapna chopimba koma tiyenera kutsegula miyoyo yathu ndi kulankhura pa zimene tikumva, pa izi ndi pamene Yesu adzathandiza Yesu anakwiya ndi chinyengo. Chifukwa chake sikuti anada anthu. Yesu amadziwa kuti ngati pali kunamizira kukhala njira ina pamene mu miyoyo ndi munjira ina sangathe kuchilitsa ife mkati monga m’mene ankafunira.

Yesu anamutcha satana ndi tate wa mabodza. Yesu ali okwiya ndi chinyengo ndipo Sali okondwa ndi ife. Izi ndi mbali ya banja – pokhala okhulupirika ndi wina ndi mzake. Pazimene tikumva ndi mmene tikuchitira. Koma muyenera kuzipereka, kwa wina ndi mzake kuchokera mkati, sindingakhale odandaula kapena yopambana. Ndikufuna kukhulupirira Mulungu kuti

angathandize ine. Koma ndi sangozinyenga kuti angandithandize ine. Koma ndi sangozinyenga kuti zonse zili bwino pamene sizili motere. Ndiyenera kuzichepesa kupeza abale abwino ndi azilongo kulankhula pa zinthu izi chifukwa pamene awiri kapena atatu ali pamodzi Yesu amabwera kudzakhala nafe, choncho ngati ndili ofuna kutsegula pang’ono mtima wanga, udidzalora Mzimu Woyera kubwera ndikuchiritisa ndipo Yesu adzakondwa. Ngati ndimanga makoma pozungulira ine ndekha ndi kufuna kukhala wamphamvu ine ndekha, pamenepo mphamvu ya machiritso ya Yesu sidzafika.

Yesu akufuna kukhala banja limene tingatsegule miyoyo wina ndi mzake. Anatiyeza ife pa malo amene tinali odzichepetsa. Yesu safuna kuti ife tikhale odandaula ndi kwidzi koma, modzichepetsa pakupempha ena kupemphera, kuthandiza ndi nzeru.

Iyi ndi njira imene banja liyenera kukhalira, koma izi sizingatheke la Mulungu m’mawa wokha. Mpingo wowona ndi banja pamodzi, monga banja lilolonse ndi banja tsiku liri lonse. Funani ndi kuyembekeza zimenezi mwa inu nokha “kwa Yesu amene akonda ine, ndidzatsegula mtima wanga kwa enanso. Ichi ndi chisankho chimene muyenera kuchita. Mungasankhe kukhala kumbuyo kwa chotchinga posatsegula moyo wanu ndi kulankhura ndi abale ndi azilongo pa zimene mukumvera. Mungasankhe kubisala kumbuyo kwa misonzi ndi zowawa kuchokera kw aanzanu. Koma mgati mungatero simudzapeza mphamvu ya machilitso ya Yesu. Adzatsenulira moyo wake kwa ife ngati tili banja Yesu adzakhala kutali mmalo mwa kusintha miyoyo yathu ndi kukhala mnjira imene afuna. Akufuna ife kugwira ntchito imeneyi pamodzi monga banja. Ndipo pamene titsegula miyoyo yathu Yesu mu mphamvu yake yonse ndi chikondi ndi ulemerero kupeza ifeyo. Koma ngati tili ndi kunyada kwambiri ndi mantha ndi zimene ena angaganize kapena kunena za ife, ndiye Yesu sadzatiyeza ndikutipatsa moyo ndi mphamvu imene afuna atipatse.

Kudya mkate wokondana wina ndi mzake

Choncho tabwera mu dzina la Yesu ndi umboni wa moyo ndi mphamvu ya Mulungu, tikufunsani kudya mkate umenewu usangowelenga, ndi kukufunsani kuti mukhale mpingo ndi banja lowona, osati kuonera. Yesu

afuna malo amene angakhalemo sakhala nyumba zomangidwa ndi manja a anthu. Amakhala mu banja, ndipo mubanja basi. Akufuna malo amene angakhale amene inu muli osati anthu wowerenga za mkate ndi kuwonera “mpingo” koma malo amene banja liri ndinu mpingo tsiku lirilonse.

Mzimu Woyera kudzera mwa Paulo anati masiku wonse ayenera kukhala ofanana. Zipembedzo zina ali ndi masiku apadera masiku “woyera” koma Yesu njira yake imodzi ndi kuti tsiku lirilonse ndi lofanana. Yesu ndiye sabata la mpumuro. Pamene tikhala mwa Ysu tsiku lirilonse, pameneposo tili pa mpumulo. Mulungu aitana inu kukhala banja . Tidzasankha kukhala banja? Ngati pali chokoma pakati pa inu mlongo muli mudzagwetsa kusamva nako? Mudzagwira bondo lawo ndi kupempha iwo kuti afewetse miyoyo yawo? Mudzapita ku phiri ndi kupemphera ndi misozi kwa iwo kuti afewetse mitima yawo? Mudzatsegula miyoyo yawo kwa iwo? Mudzapeleka moyo wanu kwa iwo tsiku lirilonse, kuzipeleka molimba, kupelekedwa onse atunthu ndi aphumphu mwa Kristo, ndi kulira mokweza kwa Mulungu pa mirakulu ya chikondi! Mudzapanga zimenezi kwa muombori Yesu? Safuna inu kuti mungodziwa za moyo wake. Akufuna kuti inu mukhale moyo wake.

Umenewu ndiwo uthenga wabwino wa ufumu. Muli mkuitanidwa mu moyo wake ngati mudzathawe kuchokera mu kunyada, kuzikweza ndi ku ulesi. Mulikuitanidwa kukhala Yesu, osati kungodziwa iye. Tsiku lirilonse kondanani wina ndi mzake kuchokera mu mtima ndi kukhuzidwa ndi miyoyo ya ena, kuthandizana ndi ana ang’ono kukhala monga Yesu tsiku lirilonse.

Uku ndi kuitana kwa Mulungu, uku ndi kukuitanani mkate wa chikondi pamodzi tsiku ndi tsiku ndipo Yesu adzadza miyoyo ndi kupanga inu tunthu monga m’mene sizinakhaleko pachiyambi. Adzachapa ndi kutchuka mantha anu ndi kuumitsidwa kwa mtima. Mtsinje wa Yesu udzathirira madzi, mu moyo ndi kukhala bwalo ya chonde. Chikondano ndi chikondi ndi Atate chidzakula kulirabe. Mudzaona nkhope yeniyeni ya Mulungu monga m’mene mukondana wina ndi mzake uwu ndi uthenga wabwino. Lero ngati mumvera mau ake, musaumitse miyoyo. Fewetsani pamaso pa Mulungu. Funani kuti tsiku lirilonse limene mutsegule miyoyo yanu kwa iwo wokuzungulirani ndipo simudzasiyana kuchokera kwa wina, chifukwa muchita izi kw AYesu muombori.

Mpingo monga banja

Mu mabanja ambiri muli mabanja eni eni amene anabadwa ndi mai ndi bambo amene timawatcha “Ana obvuta” Ana ena ali obvuta kuposa anzawo, koma ngati ali banja, ali banja, ndipo tidzathandiza kuthetsa mabvutowo. Sititenga ana eni – eni a mbanja ndi kupita nawo kuphiri ndi kuwasiya kumeneko. Timafunsa Mulungu mu nzeru kapena kukubweletsa kunyumba mu banja.

Pokuthandizani kuti mukhale ndi chithunzi cha mmene zingakhalire pamene mpingo uli pamodzi, taganizani mu kulingalira banja nyumba yanu, ndi ana amuna asanu akazi atatu ndi mai ndi Bambo. Kodi bambo ndi amene amalankhura munyumbamo? Ngati mmodzi mwa anayamata wa zaka khumi ndi zitatu ali ndi kanthu kolankhura, sangathe kunena kodi? Kodi amai sapeleka maganizo awo mu banja? Nanga kodi ana ochepe sangaongolere banja? Kodi pali ufulu nthawi zonse mbanja kwa mm’odzi yekha olankhura? Kodi pali mbali kwa ana ochepera kulira ndi kulankhura zofunika? Ziyeneranso kutero pamene mpingo wonse uli pamodzi, angakhale ang’ono angatsegule moyo ndi kulira pa chosowa, mwina mai angathandize kuthesa bvutolo ndikunena za mai wa uzimu, pamene mpingo uli pamodzi. Mwinanso bambo wa uzimu angathenso kuthetsa bvuto la mwanayo. Koma umu ndi mmene mpingo ungakhalire pamene ukumana pamodzi. Aliyense wa banjalo angathe kutsegula miyoyo ndi enawo a m’banjalo angathandize zosowazo. Izi simu msonkhano wokha. Pamene alongo ali kuchapa pamodzi pamene ali kuyimba nyimbo mu msonkhano onse, Bwanji sangathenso kuyimba nyimbo pamene ali kuchapa pamodzi?

Ngati mungalankhure ndi Atate pamodzi mu msonkhanowo, Ananso onse sangathe kulankhura ndi Yesu pamodzi pamene ali mkuyenda onse pamseu pamodzi siza Mulungu mmawa ndi lachitatu madzulo. Palibe zimene zingachitike mu msonkhano zimene sizingachitike pamene tili mkuyenda pa msewu pamodzi.

Sitidikira msonkhano kuwauza abale ndi alongo pazimene Yesu wationetsera lero. Sitidikira msonkhano kutsegula miyoyo ndi kufunsa kuthandizidwa ndi china chake. Tili chimodzi – modzi ali ndi bvuto angakhale ndi mwana wa ng’ono ali ndi bvuto angakhale ndi masiku

apadera limene aloledwa kulankhura za bvutolo, kapena adzalankhula nthawi iliyonse chifukwa pali chikondi mbanja? Uwu ndiwo mpingo wooka, pamene tsiku liri lonse tingathandizane. Palibe kusiyana pakati pa msonkhano ndi popanda misonkhano. Chifukwa timabweletsa chiphunzitso cha Yesu kwa aliyense tsiku ndi tsiku. Timalambira kuchokera pansi pa mtima ndi wina ndi mzake tsiku ndi tsiku, m'mawa ndi usiku pamene tipita kopeza chakudya, timapemphera tonse ndi kulambira pamodzi. Uwu ndiye banja la Yesu.

Penanso, pamene tikhala banja limodzi lalikulu, ngati muli kupita kumudzi ndi kumenya mkazi wanu, kapena kukhala ndi nkhanza ndi iye, Ayenera kukwanitsa kunena kwa inu. “Umu simmene njira ya Yesu pamodzi Yesu anati mwamuna ameneyu samvera kwa iye mkaziwo ayenara kupita ndikupeza awiri kapena atatu ena a mu bajja la Mulungu, ndi onse ayenera pamodzi kulankhura ndi munthu amene ali ndi nkhanza. Ndizimene anatiphunzitsa ife mu Mateyu 18, manyumba athu simalo obisalira kuchokera mu chowonadi. Sitingathe kukhala oweluzana nyumba yathu ndi kukhala osasamala chiphunzitso cha Yesu. Tsopano tili tonse banja la Mulungu ndi nyumba zathu zili za ife tonse, choncho tsopano mlongo angathe kubweletsa ena kudzalankhura ndi mwamuna wake. Sitipeputsa chiphunzitso cha Yesu mu zinyumba zathu. Chiphunzitso cha Yesu sichili cha “nyumba ya mpingo” Tsopano ali pamodzi pamene tipita ku msika kapena tipita ku zinyumba kapena pamene tipita kophunzira. Tsopano chiphunzitso cha Yesu chilli mu nyengo ndi muzochitika zosiyana siyana. Tili banja limodzi tsiku lirilonse masiku onse, usiku onse.

Kumanga njira ya Yesu

Yesu anati kuti ngati mudzafika mau anga mu wochita, pamene chimphelo chibwera (ndipo adzaima) pamenepo nyumbayo idzaima. Idzaima chifukwa inamangidwa pa mwala olimba poika mau ake mu moyo osati poganiza chabe, kapena kuimba za mau ake ngati tidzaimba za izi, Pempheleli ndi kulankhula za izi ndipo tidzasinthe njira imene timakhala pomvera mau ake wina ndi mzake, pamene mphelo idzabwera, angakhale kuti nyumbayo ndi yokongola mmaonekedwe idzagwa yonse pansi. Izi ndi zimene Yesu analonjeza mu Mateyu 7, ndiye mangani mu njira

yake, ndikuchita kanthu ndi choonadi chake. Mvekani zimenezi, ndipo mphelo sidzaonongamo.

Mu njira imene mbalame yaing'ono kapena mpira zimakhala mu miyala pamene mphelo ya mkuntho imabwera, mungakhale mu khumbi la mapiko a Yesu ngati mudzamanga munjira imeneyi ndikuloza nkhope yanu kwa iye pamene abwera, mudzakhala mu khumbi la mapiko ake. Mphelo ya mkuntho idzapita ndipo Dzuwa lowala lidzaonekera, mbalame zidzayamba kuyimbanso ndipo moyo udzakhala wa bwino ndi watsopano. Choonde mangani mu njira ya Yesu. Awa ndiwo mau a Ambuye lero.

Mmene mungadyere Mkate wookawa.

Palonso gawo lina mu Yohane 6 ananena mau amene ali olimba. Anati idyani thupi langa ndi mwazi wanga. Anayesetsa kuwauza kuti zimveke bwino. Baibulo limati anthu ambiri amene amamulonda iye anamuleka iye. Anamusiya Yesu ndi kupita kwina chifukwa sanamvetsetse ndi maganizo awo. Yesu sanawatsatire ndi kuwauza kuti anali kwa iwo kumvetsa. Anacheukira kwa ophunzira ake ndi kufunsa, “mukufuna nanaunso kukhoka ndipo Petro anati, Ambuye Yesu, muli ndi mana moyo a moyo, sitifuna kupita kwina kuli konse. Tifuna kukhala ndithu.

Yesu anafuna anthu amutsate iye amene angathe kumva ndi mitima ndi mizimu. Yesu angaika zinthu zobvuta ndi cholinga patsogolo paife zinthu zimene sitingathe kuzidziwa – mmalo mwa kupatutsa nkhoza kuchokera ku mbuzi. Anthu amene angadziwe ndi maganizo awo koma osafuna kumva ndi mizimu yawo sangathe kumutsata iye Yesu weniweni. Yesu weniweni amapanga zinthu, zachilendo poyesa mitima yathu. Ananena ndi ife za zinthu zooneka zobvuta monga “Idyani thupi langa ndi Imwani magazi anga” zimamveka molakwika ndithu, zimene angakhale Baibulo silingabvomereze kuti ndi zabwino. Chonsecho, Yesu amayesa amene amabvetsera ndi mtima ndi amene amava ndi makutu awo. Yesu amayesa amene amakonda Mzimu wa Yesu ndi amene amakonda zakunja kokha. Pali zambiri monga izi mu zambiri mu Baibulo pamene Mulungu amasiyanitsa anthu amene amamva ndi makutu awo kuchokera kwa amene amabvetsera mu mizimu yawo. Iyi ndi njira ya Mulungu, ndi imene inakhalapo muzochitika mu Yohane 6, mmene ambiri anathawa Yesu,

zapitirira mu mbadwo wina uli wonse kale angakhalenso tsopano pano. Ife sindife Mulungu. Iye ndiye Mulungu. Timazipeleka ku zinthu zimene zili za Mulungu kaya sitikuzimvetsa ndi maganizo athu kapena ai. Izinso ndi zimene zili mbuku la Yobu.

Tsiku lililonse Yesu ali kulankhula mu mkuluwiko umene uli obvuta kuumvetsa, poonetsa amene amamukonda iye mu mizimu yawo, kusiyana ndi amene amagwiritsa maganizo awo kumva bwino chabe. Ngakhalenso lero iye ali kulankhula mu mkuluwiko otero umene uli obvuta kumvetsetsa, kuti aone amene angachoke ndi ena amene anganene, “Tidzapita kuti ? mwa inu muli kuwala ndi moyo” zilinso choncho lero monga zinalili kalelo.

Yesu Mkate Mwa ife

“Ngati mukonda ine, sungani malamulo anga. Ndipo ndidzapempha Atate, ndipo adzakupatsani inu nkhoswe yina kuti akhale ndi inu kunthawi yonse. Ndiye Mzimu wa choonadi amaene dziko lapansi silingathe kumulandira, pakuti silimuona iye, kapena kumuzindikira iye. Inu sindidzakusiya inu mukhale ana amasiye, ndidzakwa inu katsala kanthawi, ndipo dziko lapansi sindiona ine, koma inu mudzandidzindikira kuti ndili ine mwa Atate wanga ndi inu mwa inu” Yohane 14:15 – 20.

Ndidzabwino, ndi choonadi chodabwitsa zimene Yesu sanapitilire kupita kwani apamene iye adali kuno ndi kuyimba nyimbo kw aiye ndi kuyesa kumvera ziphunzitso zimene anapeleka kwa ife ndiye tsiku lina kutsogoloku ndikubwera kwa ife. Zodabwitsa za chiphunzitso chake ndi choti adzakhala ndi ife mpaka nthawi yamalekezero a dziko ndipo sadzatisiya ife ngati a masiye. Anauza ophunzira ake kuti pameneiye adzabwera anthu sadzamuona iye koma inu. Ndipo timamuona iye osati ndi maso athuwa koma ndi maonekedwe a mzimu anati, mvelani ine ndi kukonda ine. Kondanani wina ndi mzake ndi kukhala amodzi monga ine ndi atate tili amodzi. Dziko silidzandiona ine koma inu mudzandiona ine chifukwa ine ndidzabwera ndi kukhala nyumba mwa inu. Ndakhala ndi inu, koma ndidzakhala ndi inu.

Sichiphunzitso chonyenga ichi, ichi ndi zoonadi, ali woona monga mu mpingo woona monga analili nthawi ya thupi. Zoonadi ndi izi Yesu anati

zidzakhala bwino kuti kupita, kusiyana ndi kungoima pamene abwelanso. Awa simau wamba kapena ndi oshashalika chabe kapena chiphunzitso chopeka. Ichi ndi chenicheni. Yesu yemweyo amene anayenda panyanja ndi kuikitsa akufa ku moyonso adzabwelanso ndikukhala mkati mwa ife mu mphamvu ndi chikondi ndi ulemerero. Sadzabwera pamene diso la dziko limuona iye koma tingakonde iye ndikupeleka miyoyo yathu pachilichonse chimene tifuna pa moyo wathu, ndikukondana wina ndi mzake kuchokera pansu pa mtima, kenako Yesu yemwewu amene anayenda panyanja ndi kutidzera pa khomo lotcheka ndi kupeleka maso kwa osaona adzakhala pakati pathu mwa ife ndi kulola ife kuti tikhale pa ubwenzi ndi iye ndi atate ndi wina ndi mzake.

Anthu ena sanaone imfa asanaone Yesu asanabweranso mu mphamvu chifukwa tsiku la pentekositi linali litangodutsa masiku makumi asanu pasaka. Anabweranso kwa ife mu masiku makumi asanu. Sanabwere kudzakhala ndi ife koma kudzakhala mkati mwa ife. Ichi ndi chinsinsi chimene chinabisika kwa zaka ndi mibadwo yonse mu Akolose 1, chopambana cha nyengo chonse ndi ichi osati Kristo ndi inu, osati Kristu kungobwera chabe kwa inu (ngakhale zili choncho) koma Kristo mwa inu, chiyembekezo cha ulemerero izi ndi za iwo amene adzakonda iye ndi kupeleka miyoyo yawo pa cholinga cha iye. Halleluya! Sadzatisiya ife amasiye ndipo ambiri sanalawe imfa mpaka adzabweranso mu ulemerero kukhala mkati mwathu. Izi ndi zimene Yesu ananena mu Yohane 14.

Mulungu Wa Dongosolo Ndi Aefenso 4

Malemia, Malawi, Africa 1996

Mfumu Yogonjetsa Ndi Mphatso Kwa Anthu

Mulungu wathu odabwitsa sanalephere kutipatsa zapamtima wake ku Mpingo wake ngati mungaone bwino ndi tcheru ku malemba, mungaone kupambana ndi zopambana za Yesu Kristo ndi ufumu wake.

Yesu anali ogonjetsa wamphamvu. Mu Efeso 4:8 imati: *“Anatsogolera ogwidwa ukaporo anapeleka mphatso kwa anthu”* (NIT) kuonetsera m'mene mfumu wogonjetsa imabwelerera kuchokera ku dziko lachilendo atapeza Golidi, Siliva ndi zinthu zina zodula kuchokera kwa ogwidwawo. *Yesu wagonjedwa adaniwo ndi kubwelerako pachionetsera cha chigonjetso atapeleka mphatso kwa anthu ake.* Mphatso zimene zaikidwa mu Afeso 4:11 - Atumwi, Aneneri, Alaliki, Abusa ndi Aphunzitsi - ali mbali ya mtunduwa Yesu pamene Yesu anakwera kumwamba mu mitambo ndi kutumiza mzimu wake woyera. Sanangoika mzimu wake kukhala mkati mwa ife amene takhulupilira. Koma anatenganso mbali ya iye mwini ndikupeleka kwa anthu osiyanasiyana amene akhulupilira iye. Yesu anali wansembe wa mkulu ndi okhulupirika mnyumba ya Mulungu yosne. Anali mtumwi, mneneli. Mbusa wabwino ndi mphunzitsi wa mkulu. *Anali uthenga wabwino kuonekera mu thupi.*

Thupi limafuna mphatso zonse

Baibulo limati pamene Yesu anapita kumwamba ndi kutumiza mzimu wake, anatenga mbali ya iye ndikutumiza zonse pathupi la Khristo, mpingo zidziwika kwa ife ndizoti ziwalo zosiyanasiyana za mbali ya matupi athu amapanga zinthu zosiyasiyana. Mungathe kuona ndi maso anu ndipo mungathe kumva ndi makutu anu. Koma simungathe kumva ndi mphuno, ndi kuona ndi pakamwa) ziwalo zonsezi sizili zofanana, mwachoncho, ziyenera kudalirana china ndi mnzake kwambiri.

Tisanapitilire ndi Aefeso 4:11, muyenera kudziwa m'mene mukufunira thupi lonse la Kristo. Timafuna tonse thupi la Kristo. 1 Akorinto 12 amati sitinganene kwa anzathu kodi “*sindili kukufuna*” m'malo mwake tiyenera “Ndili kukufuna iwe” “Ndili kukufuna iwe” uwu ndi mtima otere umene umakondweretsa Yesu kwambiri. Yesu anali ndi mphatso mwa iye yekha ndipo zina zazimenezi zili mu Aefeso 4. Mu mpingo wa Mulungu, thupi la Kristo liyenera kufuna mphatso zonsezi mwachoncho, mpingo wina uli wonse pawokha sungathe kukhala ndi mphatso zonse. payenera kukhala mlumikizo weniweni pakati pa amidzi ndi amu mzindawo mulumikizowo ndi wabwino ndi ofunika.

Galimoto lili ndi ziwalo zambiri, zitsulo, galasi ndi rabala. Iinso ndi injini, chiongolero, nyali, hutala ndi matayala. Ngati tingaika zida zonsezi za galimoto mu chipinda ndiye kuti sitidzakwanitsa kuyendetsa galimotowo, Angakhale kuti zidazo ndizabwino, sumulowa mu galimoto ndi kuyendetsa mphaka zida zonse pamodzi zitakhala m'malo mwake. Munjira ina idzakhala kuunjika zitsulo, osakhala ndi zochita zabwino. Izi zimaonetsera kufunika kwa mphatso ya mtumwi.

Mbali iyi ya Yesu - mphatso ya mtumwi, ndi mphatso imene imaona uika zinthu zonse pamodzi ndi kupangitsa “galimoto” kuyenda. Palibe Atumwi ambiri mu dziko lapansi komanso m'mene zinalili ndi zaka zambiri za chikristo.

Baibulo linasindikiza atumwi osapitilira makumi awiri ndi asanu ndi m'modzi 26 mu nyengo zonse za zaka 100. Poyambirira 12 kenako 14 atumwi ena, angakhale enawo anali ndi mtima woona ndi kukonda ntchito ya Mulungu sanali ndi mphatso yoika zinthu pamodzi mu Galimoto. Enanso popanda mphatso za atumwi, sangathe kuwona m'mene angatengere zida zina mu mpingo ndikuziika pamodzi ndikukhala mpingo wamphamvu - okhala ndi mtima umodzi, maganizo amodzi, ndi cholinga chimodzi.

Mphatso Ya Mneneri

Mphatso ya chiwiri kuikidwa mu Aefeso 4 ndi mphatso ya uneneri. *Mneneri ali othequera kuona ndi kumva fungo loipa kapena labwino.* Iye sadalira pazimene maso ake ndi makutu ake a dziko lapansi. Iye amakwanitsa kumva fungo limene lili la Yesu kapena ai. Munjira imeneyi,

mneneri amathandiza kupeleka milimo yabwino yoyenera kumamangidwa kuti Mtumwi amange. Mphatso zonse zinayi kapena zisanu zimene zatchulidwazi zili ndi malo ake ake mu thupi la Kristo, ndipo ngati mulibe mphatso zimenezi pa msonkhano pano, muyenera kugwira ntchito molimbika kumanga ubale ndi mphatso zinazo ndi anthu a mizinda ina. Mukawerenga mubukhu la Machitidwe, mudzaona kuti zimachitika pafupi - pafupi. Mphatso zimene zalembedwa mu Aefeso 4 zimayenda kuchokera mu mzinda wina kupita kwina ndikuthandiza polimbikitsa ndi kumanga, woyera mtima onse pamodzi.

Pofuna kukwaniritsa izi, mphatso ya Atumwi ndi Mneneri ndi yofunika mu mbali zisanu ndi zitanu kapena zisanu ndi zinayi mu zonse pamodzi. Popanda mphatsozi anthu a Mulungu adzakhala ndi umphawi weniweni. Ayenera kukhala amtima ofunitsitsa kukonda Mulungu kwambiri, ndikukhumudwa ndi zobvuta zina. Koma ndi kuthandizidwa ndi mphatso zobvuta zidzachotsedwa.

Kusoka Thupi La Kristo

Mphatso yamu Aefeso 4:12 ndi zofunika kukonzeketsera anthu a Mulungu ku ntchito yotumikira. Mau oti kukonzeketsera limathandauza kuti “Kulumikiza kapena kuphatikiza pamodzi” muchigiriki ndi mau amene anasankha kuthandauza kwa mphatso zisanu zimene zinali kugwirira ntchito - kuthandiza kuika fupa pa malo ake, ngati dzanja ndi losweka. Sing'anga amaika fupalo pamalo ake nthawi zina zimawawa kuika fupa pa malo ake. Koma ndizofunika kapena thupi kukhala lopunduka ndi lopanda pake. Mphatso zimene tanenazi mu Aefeso 4:12 zimalumikiza thupi la Kristo pamodzi ndikuika mbali ili yonse pamalo ake.

Kulumikizitsidwa Ndi Kudziwa Chuphunzitso

Cha Yesu

Mu Aefeso 4:13 taona kuti mphatso zimachita pamalo ali yonse - zidzatithandiza umodzi wachikhulupiriro! tawuzidwa kale mu bukhu la aefeso kugwiritsitsa umodzi wa mzimu. Mulungu akuyembekezera ife kukhala ndi umodzi wa Mzimu ndipo Mulungu watilamulira kuti tikondane wina ndi mnzake.

Mwachoncho, pali kusiyana pakati pa umodzi wa mzimu ndi umodzi wa chikhulupiriro. Popanda mphatsozi, (zonedwa mu Aefenso 4:14) kukhala mu mgwirizano ndi malo amene timakhala, tidzakhumudwa pa zokhulupirira zathu. Ndipa mphatso imeneyi imene tili okonekeletsedwa mu umodzi wa chikhulupiriro. Popanda mphatsozi (zonedwa mu Aefeso 4:14) kukhala mu mgwirizano ndi malo amene timakhala, tidzakhumudwa pa zokhulupirira zathu. Ndipamphatso imeneyi imene tili okonzeketsedwa mu umodzi wa chikhulupiriro.

Umodzi wa uzimu umalumikizidwa ndi ali yense amene anagulidwa ndi mwazi wa Yesu. Timalandira ali yense ndi kukonda amene mwazi wa Yesu unamubisa iwo. Timakonda kulandira iwo munjira imene timalandilira Yesu. Umodzi wa chikhulupiriro ndi kudziwana pamodzi za chiphunzitsa cha Yesu - zaubatizo, kuika dzanja, kulambira, kusonkhana pamodzi ndi mphatso ya mzimu. Mphatso imeneyi idzathandiza m'mene tingakondere wina ndi mnzake ndi m'mene utsogoleri uli, ndi m'mene m'Kristo ali, zoonza zake ndithu, ngati misonkhano ilibe kulumikizitsidwa ndi mphatso zisanu. Sitingakhale ndi umodzi wa chikhulupiriro, ndipo tidzasokonezedwa kuya kwa mgwirizano.

Kudzama Kwa Chikondi

Aefenso 4:13 amanenanso kuti mphatso imatithandiza ife kukhala ndi chidziwitso cha mwana wa Mulungu, chikhumbo cha Atate ndiye kuti tidziwe zili zonse za Yesu. mawu oti, “Nzeru zonse” mu malemba awa ndi “EPIGNOSIS” ndi mau amene amati ndikhale pamodzi ndi Yesu. Mulungu anasankha mawu awa ponena kuti tiyenera kukhala ndi mgwirizano weniweni wa ukwati ndi mwana wake. Awa simau enieni a ukwati ndi mwana wake. Awa simau ochokera m'mutu ai koma ndichidziwitso cha mumtima. Ndi mau omwewa amene Maria ndi Yosefesanadziwane wina ndi mnzake mphaka Yesu atabadwa ndi mau omwewa anagwiritsidwa ntchito. pamene adam anadziwa “Eva” ndipo anakhala ndi mwana.

Choncho mphatso izi zisanu ndi kwenikweni zofunikira pa mpingo. Zimathandiza anthu a Mulungu kukhala ndi kulumikizidwa ndi Yesu ndi kuyang'ana nkhope zawo kwa iye ndi kupeza mpumulo ndi mphamvu mwa iye pamene zinthu zili zolimba. Adzaphunzira kutchula dzina la Ambuye ndipo sadzachita manyazi kapena kukhukudwa.

Mau a nyimbo ina amati, “Yesu ndiye bwenzi leni leni, machimo athu ndi zopsyinja zidzatha. Tili ndi mphotho yotitengera kwa iye mu pemphero “Mphatso zisanu izi ndi zofunikira kuthandiza anthu a Mulungu kukhala mchiyanjano ndi Kristo - mlumikizitsa weniweni ndi iye kuti pamene mphepo uamkuntho ibwera osaiwala kubisala mwa Yesu. Amatembenuza nkhope zawo kwa iye ndikuona kukondwa kwa pa nkhope yake ndipo anakwanitsa kupyola mu mphepo imeneyi. Mphatso zisanu zimene zili zoyenelera kukhala ndi nzeru zonse mulumikizo weniweni wa Yesu.

Kuimba Mu Mphepo

Aefeso 4:13 imatilonjeza kuti mphatso ndi zofunika ku munthu wangwiro kumuyeso wa msinkhu wa chidzalo cha Kristo. Izi ndizothandauza kuti umunthu wathu uyenera kukhala ofanana naye Yesu ndikuti tibatengedwe ndi mphepo yoomba ya chiphunzitsa choipa chi machitidwe. Tidzakhala otheke kuima mwamphamvu, chikondi cha Mulungu. Pamene mphepo iomba modutsa ndi kugwedeza zonse zimene zingagwedezeke, noyo wa Yesu mkati mwa ife udzakwanitsa kukula ndikukhala wamphamvu. Mulungu nthawi zina amalola kuti tigwedezeke ndikutilengera ife ku zobvuta. Atate anachita izi ndi mwana wake Yesu, ndi Paulo ndi Mtumwi wina, “anabvutika mu moyo” malemba amati, “uwu ndi mwai kuti atate apeleka ife kukhala monga iye ali. Pamene mphepo ifika ndi mafunde kuomba ndi mphepo, tibatengedwe tengedwe uku ndi uko, ai. Tidzakhala amphamvu ndi mphamvu pamene tikhala pafupi ndi Yesu ndi wina ndi mnzake.

Kulankhura Mu Chikondi

Aefeso 4:15 amati kuti tidzaphunzira kulankhula choonadi ndi chikondi. Mphatso zimenezi zimathandiza ife kuti tilankhule wina ndi mnzake mu chikondi ndimnjira yowonadi. Izi ndi chinthu chofunika mu mgwirizano wa chikondi. Kulankhula choonadi muchikondi ndi kupeza njira yokondweretsa Atate ina ndi kulankhulana bwino. Tiyenera kulankhula choonadi, koma chiyenera kubvekedwa ndi chikondi, kudekha ndi kukoma mtima, ziyenera kuonekera motere mu kudekha konse. Chikondi chatu ndi kuonetsera mu mtendere ziphatso zimathandiza ife kuti tingathe kulankhulana mu chikondi munjira imene sitingathe popanda izo.

Kuphunzira Kukhulupilira Mbuye Okondewa

Malemba amanenanso mu Aefeso 4:15 kuti mphatso zonsezi zimathandiza ife kukula kufikira kumutu amene ali Kristo, Yesu ndiye mutu wa chili chonse. Ali bwana ndi Ambuye pa panyanja ndi pamtunda. Iye ali mbuye wa mitambo imene imapeleka mvula ndi mphepo imene imaomba. Ali Mbuye wa zonse zokwawa zazing'ono ndi nyama zazikulu zomwe. Alinsu wambalame za mulenga lenga, ali wa miyala yonse yokhala pamsewu. Ambuye Yesu ali mbuye wa nyenyezi zokhala mu m'mwamba ndi mwezi ndi dzuwa. Afunanso kuti akhale bwana, koma akutiitana ife kulowa mu sukulu ya Yesu kumene timaphunzira kudziwa kuti ali Ambuye. Timaphunzira kukhulupilira iye. Timaphunzira kuti ali ndi nzeru zopambana zodziwa zili zonse, ndi kuti ali ndi mphamvu zoteteza ife. Ngati sitilola iye kukhala Ambuye ndi chifukwa choti sitikhulupilira iye mokwanira kapena kuti njira zake ndi zabwino ndi chikondi chake ndi chopambana, kuti sichilephera.

Mphatso zimene zimatipangitsa ife kukula msinkhu mu ufumu wa Yesu, kuona m'mene iye ali odabwita - ali wokhulupirikira, wamphamvu, wanzeru ndi okonda. Munjira aimeneyi ndingakhulupilire iye popanga zimene iye afuna kuti tichite.

David, okondeka wa Mulungu, analemba nyimbo zambiri za chikondi kwa Atate. Atatenso analemba nyimbo ya chikondi kwa iyenso, yoti ali munthu wapamtima wa Mulungu. Cholinga chimene Mulungu ananena kuti anali wapa mtima pake chifukwa anali kudziwa Mulungu ali wabwino, wodabwitsa ndipo sanamukhumudwitse ndikumupititsa munjira yolakwika. Mulungu sanamukhumudwitse ai kapena kumuononga iye Mulungu sanamupatse mwala pamene anafuna mkate, Mulungu ali kumupatsa zonse kwa iye.

Mulungu amapeleka zinthu zambiri kwa iye ngati amayang'anira pa iye kunjira zake zonse. David amachita chili chonse chimene Atate amafunsa iye osati kuti anali omvera mouzidwa, koma anali okhulupirira chikondi cha Atate ndi anzeru kwambiri. Izi ndi zimene tonse timaphunzira ndi mphatso zimenezi. ***Atate ali odalilika ndi okhulupirika, ndiposno Yesu amapeleka mphatso zabwino, osati zoipa, kwa ana ake.*** Ndiye tingamukhulupilire iye kukhala mutu wathu, chifukwa iye ali wabwino kwa ife.

“Ndili Kufuna Iwe”

Aefeso 4:16 limati thupi lonse ndi lo “lumikizika pamodzi ndi misempha” monga momwe manja ndi miendo ili yolumikizika muthupi, mphatso zimenezi zimathandiza thupi la Kristo kubwera pamodzi kukwaniritsa kugwira ntchito ya Mulungu. Taganizani kuti thupi lamunthu silingagwire ntchito ngati manja ndi miendo zili zotayana mu malo osiyanasiyana zingakhale ziwalo zodabwitsa ndi mphamvu pazokha, koma ngati sizili zolumikizika. Kwa zina mu chikondi kulumikizika ndi mutu kuti mutu olamulire, ndiye thupi lingakhale lopanda ntchito lake.

Ndifuna kulimbikitsana inu, oyera mtima, nonse kuti muphunzire ntchito ya mphatso zimenezi ndi kuona zodabwitsa zonse zimene zikubwera ndi izo. Lolani ndi kulandira Abale ndi Alongo ochokera madera ena kukuthandizani kukhala muzodabwitsa zambiri zimene zimachitika pochokera mu mgwilizano wa mphatsozi. Ndiye tidzakhala odalilika kwa Yesu. Tingakhale okonda ndi nzeru monga Yesu ali. Tingakhale othekera pofikira anthu amene timakhala nawo, kopambananso kuthekera pokhala ndi mabanja, wokondana. Kuposanso kuthekera pokweza chikondi, ana omvera, ndi koposera pogwiritsa ntchito mphatso mu chikondi, ***chifukwa talora mphatso zisanu zimenezi mu malo amene tikhale.*** Palibe pamalo amodzi amene (sindinaone), mwachoncho Mulungu amafuna kuti tifanane wina ndi mnzake kuchokeramudzi wina ndi wina, mzinda ndi mzinda. Akufuna kuti tikule MUKUDZADZA KWA MWANA WAKE.

Maziko A Yesu

Chisitu, Africa 1996

Anthu --- osati zomanga

Baibulo limatiphunzitsa kuti Mulungu sagona nyumba zomangidwa ndi manja anthu. Efeso 2 ndi malemba ena otere amati ndife malo okhalamo Mulungu mu Mzimu Oyera – mpingo.

Timadziwa mmene mpingo wumaonekera ndiye ngati nyumba ya Mulungu ndi anthu osati nyumba, Nanga imaoneka bwanji?

Pamene muyenda muyenda mu msewu ndiye mumaona zomangidwa ndi zipembedzo ndiye poti mpingo ndi opangidwa ndi anthu osati nyumba zomangidwa. Ndiye zimaoneka motani. Tingasiyanitse motani ndi mpingowo ona ndi osaona? Awa ndi maonokedwe a mpingo umene umamangidwa ndi anthu osati miyala.

Pamene Yesu ayenda uko ndi uko kufuna mpingo woona adzadzidwa bwanji? Mpingo woona omangidwa ndi miala ya moyo umene Yesu anaukonda uyenera kukhala ndi zida zabwino. Ngati nyumba imangidwa ndi zida zoola ndiye kuti idzagwa. Ngati matabwa yogwilizana kumwamba ndi woola idzagwa pansu. Njerwa zofewa zosaumbidwa bwino kapena kuchokera ku zolakwika sizingathe kuthandiza, ndipo idzagwa. Mpingo woona umene umangidwa ndi Mulungu, osati manja anthu, ndi umene upangidwa ndi miala ya moyo - Akristo woona osati akufa. Njerwa kapena zidina ngati ndi nyumba ya Mulungu kuchokera kwa amai ndi abambo kuti ikhale yothekera. Siyenera kukhala miyala woipa (1 Akorinto 3-5)

Kuchokera Ang'ono mpaka Akulu Onse Sadziwa Mulungu

Uneneri wa chipangano chatsopano umati mpingo wa Mulungu umene ali kumanga (Jer 31, Aher8, Ahebri 10) ndiwo mpingo woona umene kuyambira ang'ono mpaka akulu onse adzadzziwa Mulungu wamoyo.

Mu mpingo wakale umakhala membara chifukwa kuti makolo ako ndi Ayuda ndiye ngati ukhulupilira chinthu chabwino ndi kuti makolo ali kumeneko ndinso iweyo umapita kawiri kawiri ndi kumapeleka chakhumi ndiye kuti membara wa mpingo umenewo. Mu chipangano chatsopanomu mpingo wa Yesu izi sizoonza ai. Uyenera kupeleka mtima wako kwa Mulungu Uneneri wa chipangano chatsopano chinali mpingo umene Mulungu akumanga Jer 3, Ahebri 10) ndiye mpingo woona ndiye kuti wang'ono mpaka wamkulu ONSE adzadziwa Mulungu wa moyo. Ngati munthu sadziwa Mulungu sangathe kukhala membala wa Yesu. Udzakhala monga zomangidwa zimene zili zofewa kapena kuwola – Nyumba imene Yesu akumanga ndi nyumba yopambana ndipo Yesu adzagwilitsa ntchito zida zabwino zokha pomanga nyumba imeneyi.

Osanyengelera

Machitidwe 3 imati Yesu anali Mneneri ndipo anamanga nyumba yake (Mpingo) ndipo ali yense amene samvera iye adzachotsedwa pakati pa anthu. Izi ni zimene Yesu analankhula mu Mateyu 18 kuti ngati munthu apitirira kuda mnzake. Kuuma mtima kuzikonda ndikupitilira kumwa moyo, kukalipira mkazi kapena ana ndikuchita zakuba mu malonda awo, kunama kapena ulesi ndiye tipita kwa iwo ndikuwatandiza, mwachoncho ngati sasamala pakumvera chiphunzitsa cha Yesu ndiye tiyenera kubweretsa awiri kapena atatu ena ndi kulankhura ndi munthuyo. Ngati sakumevlanso pazimene Yesu anena ndikuti sakusintha, ndiye tilankhure ndi mpingo wonse ndi kumufunsa kuti achoke.

1 Akorinto 5 limati tiyenera kuchotsa isiti kuchokera pa chakudya. Yesu anatilamulira osadya kapena kukhala pamodzi ndi munthu amene sadzasintha moyo wawo ku chiphunzitsa cha Yesu. Pasakhale chigwilizano ndi iwo, ndikuti achotsedwe pakati pathu. Baibulo limatero “Yesu ndi omanga wamkulu. Iye sadzamanga ndi zofewa ndi zowola akufuna kumanga nyumba yapamwamba kuti akhalemo - imene ili yoyenera Mfumu monga iye.

Kusankha Zida Zomangira

Choncho zida zomangira mu nyumba ya Mulungu ziyenera zapamwamba, izi sizoti munthu ali yense ndi wabwino ai. Sizoti munthu ali yense ndi wabwino ai. Koma, zithandauza munthu, akonde ndi kumvera Yesu ndipo sanyosera kuthandiza kwa ena, amene afuna kuthandiza iwo kukonda ndi kumvera Yesu, afuna kuthandizika zomangila zabwino za nyumba ya Mulungu ndi pamene munthu amene safuna chithandizo iye amati, “osandiweluzana ine” “samala zako amaziteteza,” “chotsa choipa m'maso mwako” zimenezo ndi zomangila zoipa, zimene Mulungu salora mnyumba yake. Yesu sadzamanga nyumba yake motelo. Iyi ndi mitengo wowola ndipo udzadulidwa pakati pa anthu. (Machitidwe 3:23, Mat 18, 1 Akorinto 5) Mu mpingo woona amene atelo saloledwa. Ngakhale atakhala ndi ndalama zochulukana, kapena amadziwa Baibulo motani angakhale mtsogoleri” koma ngati sabvomeleza mpingo wa Yesu mofewa ku chiphunzitsa cha Yesu, ndiye sangakhale ku mbali ya mpingo woona umene uchitika mu mzimu. Ngati akana, chikondi ndi kupepsa nzeru, kuthandiza ndi kudakha mtima, ndi kuwalola kukhala pakati pa abale ndiye tikutsutsa Yesu ngakhale malamulo ake.

Yesu adzamanga ndi zida zomangira zabwino, ngati tili ndi mitima wofewa, kukonda chiphunzitsa chake, kwenikweni tifuna kusintha zinthu mu moyo wathu umene ufunika kusintha, ndikubwera ndi nkhope zathu kwa iye munthawi ya zobvuta kapena kuyesedwa. Kumufuna iye ndi abale athu kuthandiza ifeyo. Ndiye kuti mwala yamoyo yokongola kumangira yomangidwa ndi nzeru.

Nyumba Yomangidwa Ndi Nzeru

Nyumba, tikutenga zomangira zonse zimene zili zoyenelera kumangira nyumba. Miyala yonse ndi matabwa onse ndi zida zonse zimene Yesu wazisankha pa nyumba yake. Tsopano zonse tiziike malo amodzi - ndiye kuti tilibe nyumba. Nyumba ya Mulungu imafunika kuposa mitengo wabwino yokha. Simungathe kugona mnyumba imene zida zake zangoikidwa pamalo amodzi sizidzakupulumutsani ku mphepo ya mkuntho, angakhale ndi zomangira zapamwamba.

Palinso njira imene tingamangire nyumba ndi zida zabwino - njira imeneYesu afuna pogwilitsa miyala ya moyo. Monga mmene

achipembedzo chomwecho mpingo woona umakhalir sumangidwa ndi miyala, koma anthu, miyala ya moyo. Ndipo iyenera kuoneka ndi maonekedwe ena kuti ikhale nyumba ya bwino yoyenera kukhala Yesu.

Palinso njira ina yomangira nyumba kuti yosabvuta kukhala komanso mphepo osaigwetsa. Yesu ndi omanga wa nzeru ndipo amanga nyumba motere; Ndikuuzani maonekedwe anyumbayo chifukwa ngati sitingamange motere nyumba idzagwa pamene mphepo idzabwera ndi mmene tingamangire nyumbayo ndi zomangira zapamwamba ndithu zida zoipa ndi zosaloledwa mu nyumba imeneyi pokhapo pali kusinthika ndi kukhala zida zabwino monga Yesu afunira.

Mnyamata olemera anauzidwa kuti anali wabwino. Koma sanali oloedwa pa nthawiyo chifukwa anali ndi umbombo mu mtima mwake. Anali kudalira ndalama zake koposa Mulungu, anali wa chisoni kupeleka ndalama ndiye Yesu anati, “Sungakhale ku mbali ya Mpingo munjira yotere mpaka mutasintho moyo wanu. Simuli oloedwa kukhala miyala ya moyo mu nyumba yake, umu ndi mmene Yesu ali kumangira nyumba yake. Amationa ife ndi kutikonda ife monga adachitira ndi munthu uja komanso akatiuza kuti tisinthe. Ngati sitingasithe, potipabe ife chikondi ndi malonjezo onse anatipatsa sadzakwanitsa kutigwiritsira ife ntchito monga mwala wa moyo. Adzatiika pambali mpaka nditafewetsa mtima yathu.

Kusendeza Pamodzi Monga Amodzi

Ndipamene miala ikhala pamodzi ndi kulumikiza ndi moyo wa tsiku mu chikondi ndi kupezana ndi kumanga ndi makonzedwe a Mulungu. Mulungu akhalidzamo

Ndipamene miala yonse ikhala pamodzi ndi mamangidwe ndi makonzedwe amene tonse tingakhale ngati kwathu. Zimenezi ndi zoonza kwa Yesu. Nyumba ya Yesu imangidwa ndi mamangidwe ake ndithu osati athu. mamangidwe ake ndi oti abambo zana, Amayi, Abale ndi alongo. Makonzedwe ake ndi kuti tichitsilike. Makonzedwe ake ndi oti titengeleni zobvuta ndi kukwanilista lamulo la Kristo. makonzedwe ake ndi oti tikhale pamodzi monga iye ndi Atate ali - Amodzi monga tikaona Timu, mwaonanso David mukaona mwana mwaonanso atate. Yesu anati

tidzakhala amodzi monganso iwo ali tiyenelanso kukhalanso otere osati miyala yosiyanasiyana ndi kubwera pamodzi la Mulungu, koma banja lomangidwa pamodzi tsiku ndi tsiku.

Uku ndi kumanga kwa Yesu Mphepo idzabwera ndipo nyumbayi yidzaimabe. Yesu adzabwera ndi kukhala pa nyumbayi ndipo idzabweretsa iye kukondwera ichi ndi chifuniro cha Mulungu kwa anthu ake mu dziko lili lonse, ndipo tikuitanani ku zinthu izi mwa changu.

Atate Chikwi, Amayi, Abale, Alongo

Atate chikwi, Amayi, Abale, Alongo Yesu anati ngati mundimvera ine mudzakhaladi atate chikwi Amayi, Abale, Alongo osati chikwi cha okhala pafupi koma chikwi cha abale apa banja. Ichi ndi chifuniro cha Mulungu. Ichi ndi chiphunzitso cha Yesu kuti amange ndi zida zabwino. Zida zoipa sizololedwa ngati sizisintha. Nyumba ya Yesu ndi yomangidwa ndi mamangidwe ake osati athu ndipo mamangidwe ake ndi Atate chikwi Amayi, Abale, ndi Alongo mamangidwe ake ndi oti tiyenera kuwulura machimo kwa wina ndi mzake kuti tichiridziwe manangidwe ake ndi yoti titengelane zothobwitsa ndi kukwaniritsa lamulo la ambuye. Manangidwe ake ndi oti tiyenera kukhala amodzi woti ukaona Timu wawonanso Devedi. Ukaona mwana wawonanso Atate. Yesu anati tiyenera kukhala amodzi monga iwo ali ifenso tikhalenso munjira yotereyo osati miyala yosiyana imene imabwela la Mulungu koma banja lomangidwa pamodzi tsiku ndi tsiku.

Kubweretsa Chokoma Kwa Yesu

Ngati pali zosintha zina zimene zili zofunika kuchitika. Yesu anati “Ngati undikonda ine” mudzasunga malamulo anga” ndiye chonde sinthani pazimene Yesu akuitamilani. Musaope ai, Ambiri safuna kukonda chikondi ndi choonadi ndipo adzakhala okwiya ndi zinthu izi chifukwa ali ndi zinthu zobisika mu moyo wawo, njira yoona ya Mulungu imakhala yokanidwa ndi Satana, Mdani.

Ndiye limbikani, pililani ndi kudekha mu zinthu zonse izi, wonetsani chikodni kwa Yesu pakuchita chili chonse chimene pa chiphunzitso cha

Yesu. Pepani abale ndi alongo amene kungathe kukhala nawo, pemphelani ndi iwo lankhulani ndi iwo. Onongani zopinga pakati pa abale ndi alongo, zopinga za mantha ndi kunyada, zopinga za ulesi kapenda zochititsa manyazi, zopinga za ulesi kapena zochititsa manyazi, zopinga za manyazi, zopinga za chiweruzo, tengani zonsezi ndi kuchapa zonse pachifuniro cha Yesu. Phunzilani kukondana wina ndi mnzake tsiku ndi tsiku. Izi sizidzangobweretsa Yesu chimwene chokha, chifukwa choti ndi mamangidwa a mpingo wake, koma sizidzasintha moyo wanu kopambana muyeseni Ambuye lero, zinthu izi ndi zoonza.

Kwa inu a Kristo woonadi, amene muli ndi mzimu woyera wamoyo inu, tsiku lina, sitidzakhala ndi chilankhulidwe chosiyanasiyana. Matembelero a Babelo adzaonongedwa, miyala yonse ya moyo idzakhala ndi kuthekera pokhala ndi kulankhula ndi mgwirizano odzaza wina ndi mnzake.

Nyumba Ya Mulungu

Komba, Malawi, Africa 1996

Banja La “Thanzi” - Mkwatibwi Wokonzeka

Posachedwa, Yesu abwera chifukwa cha mkwatibwi wake. Bayibulo likuti Yesu adzabwelera mkwatibwi yemwe wadzikhonzেকেletsa yekha. Kodi tingayikidzike bwanji miyoyo yathu kukhala yokonzekera? Chabwino, lingalirani chithunzithunzi ichi ndi ine.

Pamene zipembedzo zathu kapena uzimu ukachitika pamalo patsiku limodzi musabata, ndiye dzili ngati kudya chakudya chimodzi sabata iliyonse. Umu simomwe atate anati tikhale. Tayenera kudyetsa matupi athu tsiku lililonse kuti tikhale. Anapangisanso mizimu yathu kudya nthawi zambiri musabata – kudya mkate wochokera kumwamba ndi kukondana wina ndi nzake tsiku, ndi tsiku, ndi tsiku. Anatipanga kukhala mu ufumu wa ansembe pamodzi ndiku bweletsa mkate wamoyo kwa aliyense pamene tikudzukira m’mwamba, pamene tikukhala pansu ndi pamene tikuyenda munjira.

Kupembedza kwa Yesu kuli ngati kudula nkhuni ndiponso ngati tichapa Malaya pamodzi. Timaphunzisana mau a Mulungu mumalo a miyoyo yathu. Pamene tiyenda mu misika pamodzi. Ngati tiona munthu amene ali wovutitsa mkazi wake, timamubweretsela mawu a Mulungu ndikuyamba kumuthandiza kuona Yesu. Pamene tiona mwamuna kapena mkazi amene ali wozikonda ndi zimene alinazo. Timawakonda ndi mau a Mulungu tsiku lililonse. Sitidikila wina ku “lalikira uthenga” okhunzana ndi izo la Mulungu, koma timawapatsa mau a Mulungu chifukwa tonse ndife a nsembe.

Mwana wang’ono amene amadya chakudya chimodzi sabata iliyonse akhodza kudwala ndi kufowoka. Izi ndi zowona za mkwatibwi wa Yesu. Tayenera kudzyetsa tsiku ndi tsiku ndi utsiku, tsiku ndi usiku – kuti tikule a mphamvu. Timadyetsana mau a Mulungu. Timapembeza limodzi tsiku lililonse. Timamufunsa Mulungu kuti atithandize tsiku lililonse.

Anthu ambiri atha kuganiza kuti banja la thupi lingadwale kwambiri ngati lingamasonkhane la Mulungu ndi la chitatu lokha lokha. Mu bayibulo,

tikuwerenga dza banja la Mulungu ku Machitidwe 2. Akunena bwino bwino kuti adali pamodzi tsiku lililonse ndipo amadziperereka tsiku lililonse kudziphunzitsa za atumwi, kutumikirana m’modzi ndi nzake. Ndikupemphera limodzi. Tsiku lililonse, usiku uliwonse. Samadzitengela zomwe alinazo ngati zawo. Adanyema mkate ndi kudya limodzi mumanyumba awo tsiku lililonse.

Tidanzidwa zaka zambiri kuti chikhristu ndi mpingo ndi chinthu chimene tingochionerela ndikubwereranso ku moyo wa kale linja. Tili ndi mayiko awiri kapena atatu osiyana. Tili ndi dziko la kunyumba kwathu ndi banja, dziko la ku ntchito ndi kukhala, ndi dziko la “mpingo” wathu. Yesu wathu adatiphunzitsa kuti mayiko onsewa ali pamodzi ndiponso ali chimodzi. Aliyense amene wapereka miyoyo yawo kwa Yesu ali ndi dzana (100) la atate, azimayi, abale, alongo, malo ndi zinthu – osati dzana la anthu. Oyandikana nawo ndi okuwadziwapo ena, koma dzana la amayi ndi abambo. Izi ndi zomwe Yesu adatiphunzitsa. Ichi ndi chomwe mpingo ukuthandauza. Tsimalo opitako, koma chomwe tili tsiku lililonse. Mpingo uli ngati kukhala pamodzi ndi pafupi ndi wina ndi mzache ngati mayi ndi mwana wongobadwa kumene. Awa ndi mau eni eni a Yesu.

Zotsinga

Sono chimatipangasa kuti tidzitsiye zinthunzi ndi chiyani?

Chotsinga choyamba ndi chiphunzitso chotsamalizika chomwe tidaphunzitsika dzaka zapita zambiri. Koma chomwe tikazindikira ziphunzitso za Yesu zokhudza zinthuzi. Pali zotsekereza kapena zotsinga zotipangitsa kutsiya njira yomwe Yesu afuna kuti tikhale ngati mpingo. Ngati tikhala odzikonda kapena aulesi. Sitikufuna kukhala mpingo womwe Yesu afuna kuti tikakhale. Tikufuna kukhala moyo wathu m’mene tafunira kukhalira. Ngati wina abwera kwa inu kapena kwa ine ndi kubweretsela uthenga wa Yesu za momwe tikukhalira ndi akazi athu kapena amuna athu. Munthu wozikonda amati, “dziwa zako. Pitani kutali ndi ine.

Koma iyi sinjira ya Yesu akuti, “Aliyense amene andidziwa ndi kundikonda ine akonda dziphunzitso zomwe ndi phunzitsa.” Wokond Yesu adzanena “Dzikomo kwambiri chifukwa chondithandiza.” Ndikufuna kumudziwa Yesu kwambiri. Ndinali wosaona koma mwandithandiza kuonanso

pang’ono, ndikuthokoza pa ichi.” Umu ndi momwe banja la Mulungu layenera kukhalira pamodzi tsiku lililonse. Timathandizana kudziwa bwino Yesu pothandizzana kusiya tchimo, kondanani wina ndi nzake, ndi kusamalira monga tidzisamala ife eni. Izi ndi ziphunzitso za Yesu. Umu ndi momwe adakhala moyo wake ndi ife, ndi momwe watiyitanila kukhala moyo uwu ndi wina ndi mzache. Umu ndi momwe mkwatibwi wayenela kukhonzekera kubweranso kwa mkwati Yesu.

Ichi ndi chifunilo cha Atate kuti “tisakhuze mkwatibwi” koma kukhala mkwatibwi. Titha kupanga ichi ngati tikondana ndi kusinthana miyoyo ndi wina ndi mzache tsiku ndi tsiku. Izi zipotsa kuti “Hi!” ndi kuti “ndimakukonda!” ndi kamayenda. M’malu mwake. Nditsekula mtima wanga kwa iwe ndikukufunsa kuti undithandize. Ngati muona tchimo m’moyo mwanga, simupita njira yina ndi kuyisala. Inu ndinu a kazembe ake a Yesu monga momwe Mulungu amandiuzila kudzera mwa inu.

Uwu ndi mpingo – kukhala moyo uwu tsiku lililonse, osati kupita ku nyumba ya Mulungu, koma kukhala malo omwe Mulungu amakhala. Ndiye manyumba athu, m’malu ogwilira ntchito athu ndi mipingo yathu yonse ili limodzi, ndi yayikulu. Palibenso zotsekereza kumtima wanga ndi wanu komanso dzotsekereza kunyumba kwanga ndi kwanu. Ndikutchosa kudzikonda kwanga ndi kudzikuzi, ndikuchotsa ulesi wanga ndi kusakhulupirira ndipo ndikukonda ena ngati momwe Yesu adandikondera. Ngati wina aliyense achita izi, kuchokera ang’ono mpaka aakulu, Yesu adzathira mafuta amachiritso ndipo ife ndife mpingo ndi mkwatibwi wokongola. Ngati sitidzafuna kukhala nawo m’mawa wa tsiku la sabata, ife tidzasemphana ndi mtima womwe uitana za Mulungu, ndipo tisakhale zipembezo zomwe zili zopanda phindu.

Utsogoleri M’nyumba Ya Mulungu

Kumachitidwe 20, Paulo amalankhula kwa atsogoleri ena ndikuti, “ndali Mzimu Woyela womwe adakupangitsani kukhala wamkulu woyang’anira.” Izi ndi zotsiyana ndi njira ya munthu. M’mayiko ambiri omwe takhala tikupitako, njira yomwe munthu amakhala mtsogoleri m’nyumba ya Mulungu ndi pokha pokha apita ku sukulu ya dza bayibulo kapena ku seminare, kapena awerenge kupotsa momw anthu

ena amgathe, koma zonsezi ndi zifukwa zosayenera. Izi si njira zomwe Mulungu amapangira atsogoleri.

Padali nthawi zomwe takhala tikuyenda mumipingo yosiyana siyana muma tauni ndipo tidafunsidwa kulankhula ndi atsogoleri. Panthawiyo, padali njira ziwiri zomwe tidaganiza omwe ali tsogoleri. Njira yapafupi ndiyoganiza kuti, “Kodi amene ali mu utsogoleri ndi ndani, kapena kodi ndi ati amene adatsankhidwa ndi anthu kukhala atsogoleri?” chabwino atsogoleri ndi okhawo amene amakhala ndi a maudindo awo, mwa chisanzo “Abusa kapena abusa aakulu”.

Koma umu ndi momwe Mulungu amasankhira atsogoleri ake. Sadasankhe anthu chifukwa cha sukulu ya baibulo kapena seminare. Adasankha anthu momwe adaona mumitima yawo ndi kuona kuti adali okonzeka kusiya machimo awo ndi dzikhumbo khumbo pa moyo wa munthu ndi kumtsata pokhapokha iye kuwapulumutsa iwo dzingavute maka. Sono, ngati tafunsidwa kulankhula ndi atsogoleri muma tauni kapena mumayiko osiyana siyana. M’ malo moyitana aliyense amene ali ndi udindo kapena m’maina kuti abwere, talankhula kuti, aliyense amene apita kukagona napempherela anthu oyela mtima, amene masana amasamala oyera mtima ena ndi ena osakhulupirira, amene ali ndi mtima womusata cholinga cha Mulungu mu dziko, amuna kapena akazi, ang’ono kapena akulu, ngati musamalira mizimu ya anthu ena osati pa inu nokha, ndiye kuti ndinu mtsogoleri. Bwerani tiyeni tilankhule umu ndi momwe mzimu woyera umapangira oyang’anira aakulu. Izi dzikusiyana kusankha mtsogoleri kamba ka udindo kapena maphunziro.

Machitidwe 6, padali ntchito yaikulu yochita ku Yerusalemu. Sadanene kuti sankhani anthu awiri amene ali ndi seminare yamaphunziro ndi kutsogolera bwino kapena kulankhula bwino kusiyana ndi ena.” Iwo anati, “sankhani anthu asanu ndi awiri mwa inu amene ali odzazidwa ndi mzimu woyera ndi nzeru.” Mukuona anthu achikondi ndi anthu othandiza moyo wawo wa tsiku ndi tsiku. Awa ndi amuna ndi akazi amene Mzimu Oyera ukuwadzutsa. Sidzitengera pepala lamaphunziro lomwe aliyika pakhoma ndi chizindikiro cha golide. Dzimatengela mtima wosweka ndi chizindikiro cha Mzimu woyera. Sono izi ndi ziphunzitso zina za utsogoleri, chifukwa Mulungu akufuna kusankha adzitsogoleri pa anthu onse.

Zomwe munthu amaganiza kuti ndi zofunikira, Mulungu saganiza choncho. Pamene Samueli amafuna kusankha munthu wokhala mfumu, ambiri adzibale a Davide adaoneka kuti adzakhala atsogoleri abwino. Koma wang’ono, kanyamata kabusa nkhusa kadali komwe Mulungu adasankha, tsalabada za mkati mwa mbale kapena mlongo. Amaona za bwino ndi ukulu wa mtima wa munthu ameneyo. Davide amafunitsitsa kuteteza moyo wake ndi wa nkhusa zake ku mkango ndi dzi mbalangondo. Davide ali wang’ono adapha mkango ndi chimbalangondo kuti apulumutse kankhusa kamodzi ka Mulungu. Davide adamuza Sauli “ndapha mkango” ndapha chimbalangondo ndithanso kupha Goliyati.” Chifukwa a Davide adali wodzipereka kupulumutsa nkhusa, Mulungu adaona kuti Davide athanso kupereka moyo wake pa ana ake. Ichi ndi chizindikiro cha mwamuna ndi mkazi chomwe Mulungu adzutsa kukhala mtsogoleri, osati mwamuna kapena mkazi omwe adachita bwino mumaphunziro, koma munthu yemwe adzazipereka moyo wake pa nkhusa za Mulungu.

Bukhu la Machitidwe likulankhulanso za Davide kuti adali wakufuna kwa Mulungu chifukwa amachita zonse zomwe Mulungu amafuna. Davide adalakwa m’ moyo wake, tikudziwa zimenezi. Koma mtima wake udali woti akachite zonse zomwe Mulungu anena. Pa chifukwa chimenechi Mulungu amapungulira mafuta an’ dalitso pa iye ndi kumuvomereza Davide kukhala mtsogoleri pa anthu ake – chifukwa amdzipereka moyo wake pa nkhusa za Mulungu ndi kuchita zonse zomwe mbuye wafuna kuti akachite. Ichi ndi chikondi cha Mulungu: Amuna, Akazi ndi ana amene adzapereka miyoyo yawo pa nkhusa za Mulungu, ndi omwe adzachite zonse zomwe Mulungu adzanena, omwe adzachite zonse zomwe Mulungu adzafunse – iwo ali amuna, akazi ndi ana omwe ali akumtima wake wa Mulungu. Ameni?

Mtima, Moyo, Maganizo Ndi Mphamvu

October 1999, AFRICA

POSACHEDWA, ndinalankhula ndi atate zatathauzo lakukonda iye. Kukambirana kwithu kunali kukhuza ine. Kulingana ndi mutu wakukonda iye kuchoka pa mtima wabwera kulingana ndi nyimbo imene mbale anayamba kale. Ndikumva ngati ndinene zimene iye anayamba kuphunzitsa ine posachedwapa. Ngati ziri choncho, ndifuna ndigawane nanu zimene Mulungu wawonesela ine zokhuza kumukonda iye.

Ndidziwa tonsefe lamulo lalikulu zikupanga nzeru kwa ine kuti ngati sitimvera lamulo lirilonse tisayambe ndikusamvera lamulo lalikulu. Inde popeza sitifuna kusamvera malamulowa ingakhale limodzi la iwo; koma limene anena Yesu ndi lalikulu pa onsewa ndilofunika kuliona ndi chidwi chachikulu. Nditafunsa atate tanthauzo lake lakukonda iye, anandikumbutsa za lamulo lalikulu, anandifunsa kuti ndigwirizane naye zatanthauzo la lamulo lake.

Mulungu anati timukonde ndi mtima wathu wonse, timukonde ndi moyo wathu wonse, timukonde ndi maganizo athu onse, timukondenso ndi mphamvu zathu zonse. Tikaganiza tonse pamodzi za tanthauzo la zimenezi, ndinaganiza ndikulemba za izo; ndinapanga izi mwa ine ndekha, ndi chiyanjano changa ndi iye; ngati mufuna tikhoza kugawana zomwe tidakamba.

Mtima Wathu Wonse

Pamene iye anati timukonde ndi mtima wathu onse. Panali zinthu zapadera zimene iye anali kutanthauza. Kutanthauza kuti tizipeleke kwa iye mwatunthu. Safuna mpikisano pakudzipeleka kwa mtima wathu; ngati ndi mvera lamulo lakukonda iye ndi mtima wanga wonse; ndisamalize ndi mtima wanga wonse. Ndipange chisankho cha mtima wanga. Tonsefe timasamira pakuzipereka za zinthu zosiyanasiyana.

Anthu ena amazipeleka pakudya zinthu. Mumayoko ena, kuzipeleka pa chakudya chiri chinthu chofunika kwambiri. M'dziko la itale, mwa chisanzo amanunkha chakudya ndi kuti ziri bwino amachipatsa ulemu chakudyacho ndikuchikonda zedi; ndi kukonda kununkhila kwa chakudya.

Mulungu anati sindizakonda kuti ukhale osusukira chakudya mu mtima mwako (mtundu wa chakudya chotere) ndi kuti kodi ichi sichodabwitsa chakudyachi ndi chingwiro, chikumukhila bwino, ndi chodyeka bwino. Chakudyachi chiri chokongola m'maonekedwe. Mulungu wati iyayi usazipeleke pa zinthu zopirira, anthu akutayika za zimenezi Mbuye anati, ndifuna uzipeleke kwa ine, osati pachakudya, chakudya m'chabwino koma usazipeleke mwatunthu ku icho.

M'maiko ena, mdzikhaliwe, zathu mpingo saunvetsa, ndipo kuti mpingo si banja leni-leni. Anthu anapeleka mtima wawo ku mabanja a thupi. Taonani, ili ndi banja langa, mmalo mopeleka mtima wanga kuzimene Yesu ananena kukhuza athu a Mulungu ngati banja lake, amakhala ndi chidwi chapadera dera anakhalanso ndi Nsanje ya banja anthu awa ati ndidzina langa lotsiliza la ine.

Anthu awa awoneka ngati ine – Abambo anga, Amayi anga ndi Ana anga. Amalora chakudya, mwazi, chinyengo, chikhale chosusa mzimu wa choonadi wa khristu ndikutuiza tanthauzo leni leni la banja pamene ife tabadwa mwatsopano. Yesu amati chiani za ichi? Azimayi zana abale ndi alongo, amayi anga ndani? Abale kapena alongo? Amene achita cholinga cha Mulungu basi.

Anthu ena a chipembedzo a ali ndi mtima wokonda banja lawo la thupi basi munjira yopusisa athu kuti asaziwe m'mene tiyenera kukhalira moyo wosangalasa Yehova.

Ngati ziri m'mene tionere ife zokhuza banja tisamale banja lathu la thupi; ndife oipisisa kuposa anthu osapemphera. Mawu amati, ndithu tikonde akazi athu, amuna athu ndi ana athu. Koma mtima wanga akazipereka pa ichi ndikupatsa khungu anthu ena ndiye zingokhala kuti ine, ine, ine! Uku ndikulakwitsa kwakukuru. Mtumwi Paulo anati kwa ife ndi Mzimu amane anali ndi akazi akhale ngati alibe, umu ndi m'mene mawu anenera. Mawu sakuti, musawakonde akazi anu ndikuwasamala chimodzi amuna anu ndi ana anu. Mulungu anati, ndiri ndi nsanje ndi kudzipereka kwa

mtima wako. Mulungu akuti uzipeleke mwatunthu kwa ife. Kenako ndisazigawa kwa anthu ena tisakhale eni ma banja ndilatengedwa ndi iwo monga a khungu.

Mitima yathu ili ya kwa Mulungu, mitima yathu yonse.

Ndaonapo anthu akuzipeleka kuzinthu zopusa; amangoyenda mtunda wopanda chirichonse.

Akhoza kuyima pa nyanja ndikuyang'ana mafunde chifukwa amakonda kuona madzi. Muganiza za ine ndi chilengedwe changa. Musataye chikondi chanu ndi kuzipeleka kwanu pa zinthu zonse ndinalenga.

Anthu ena amazipeleka ku zinthu za dziko. Amakhala ndi nsanje pa dziko lawo. Mukaonera mpira, kapena kanema, pamakhala mpira wa dziko lonse, dziko ndi dziko kusewera mpira. M'malo amenewa anthu amaima chifukwa timu yawo yalephera. Ambiri amakhala ndi chimwemwe pamene timu yawo yapambana.

Mulungu anati, iyayi mtima wanu ukhale kwa ine basi. Usapeleke mtima wako ku zinthu popanda pake. Ukhoza kuonera moira, ukhoza kukondwera pamene timu yako ipambana, koma kulira ndi kukondwa usiyire ine atero Mulungu.

Mulungu wati afuna, mtima wathu wonse, ndikaona zimenezi kubwera mtima wanga, kaya ndi pachakudya kapena pa banja, kapena pamasewera a mpira, ndiope Mulungu basi, ndisazipereka pang'ono ku zinthu za iye.

Iye anati, ndifuna mtima wako wonse, ndifuna kuzipereka kwako konse kwa ine. Ili ndi lamulo, choncho ndichite chimenechi ndikaona mtima wanga ukufuna zina ndi bweze kuti ulowele kwa ambuye basi. Ndilamulo choncho, chisankho chimene ndingapange chikhale chotere. Ndiziperekeletu kwa iye basi osati ku zinthu zina ayi.

Moyo Wathu Wonse

Chinthu chinanso ndi chakuti “Moyo wanga wonse” ichi chitanthauza zinthu zambiri. Zikuchitachita ndi mawu woti (kuzikuza) zichitechite ndi zinthu zimene muli chizindikiro changa. Ine ndine ndani? Kapena ndiganiza kuti ndine ndani? Uwu ndi moyo wanga. Ndakangalika pozilora

ndekha kunyadira pa zinthu zimene ndakwanilitsa. Ndachita zazikulu mu malonda ndipo ndikumva bwino pa zimenezi. Ndikuchimva kuti ndine odala ndikumva bwino ndikuzimverera ndekha kuti zanga ziri bwino. Ndine waukhondo ndipo zanga ziri bwino. Ndine wochenjera ndipo zanga ziri bwino. Ndikhonza kupangisa anthu kuseka.

Ndikhonza kunena nthano kapena nkhani ndikumva bwino pazimenezi. Ana anga ndimawasamalira, kuposa anthu ena ndimamva bwino pazimenezi. Ndiri ndikusunga kwa zinthu kuposa mmene eana achitira, choncho ndimamvanso bwino. Sindigonja, ena amataya mtima, koma ine ndine wamphamvu, ndipo ine sindigonja.

Uwu ndi “moyo wanga” ndipo uku ndikulakwa kwakulu pamaso pa Mulungu kukhuza zinthu zotelezi makhoza kulingalira zambiri. Kumbukirani m'mene satana anachotsedwa kumwamba. Satana anali ndi mzimu woti ine, ine, ine nthawi zambiri. Sanaphe mngelo kumwamba. Iyeyu sanaze katundu wa mngelo aliyense. Koma anali ndi maganizo oyipa. Anaganiza za yekha osati Mulungu.

Iye anati, ndine wokongola, ndizakwera nakhala ngati wamkulu kulu. Ndili nayo mphatso yakuyimba, ndipo ndinawala kuposa miyala yamtengo wake, ndiri nawo ufulu woonedwa kuti ndilipo komanso wofunika.

Ndiri nawo ufulu woti anthu aziziwa kuti ndilipo, komanso kutcheleza kwa ine chifukwa ndine wofunika, ndiwapadera ndili ndi uzimu kuposa angelo onsewa.

Mulungu anati, ndakuchosa pakupezeka kwanga Mulungu akuti, undikonde ine ndi mtima wako wonse, uchengetere mtima wako ndi moyo wako, kuti undipembeze ine ndikundikonda ndi moyo wako wonse.

Mtumwi Paulo anati, ndiri nazo zoti ndikhoza kunyadira, koma ndiyenera kuti ndinyadire mwa Yesu ndi iye wopachikidwayo. Ndapachikidwa ku dziko ndipo dziko – lapachikidwa kwa ine.

Iye anati, ine ndine wamkulu wawo chimwa ndine woipitsisa ndi wochepetsa mwa iwo wokhulupira Mulungu. Ndinyadire muzopeka zanga, uyu anali Paulo Mtumwi amene anli munthu wabwino. Koma anapanga chisankho chokonda ambuye, ndi mtima wache wonse anakondanso Mulungu wache ndi moyo wache wonse. Sananyade

chifukwa chazimene iye anachita kapena m'mene iye anakhalira muzochita zache.

Munthu ameneyu (Paulo) anapita mmwamba nthawi yina kumene Mulungu anakhala. Koma sanafune kunena za zonsezi, iye anati, ndiziwa munthu amane zaka zambiri zapitazo sananyade, ine ndine Paulo mtumwi, ine ndinapitako kumwamba. Anali wozichepesa kuti alankhule zimenezi sanafune kuzisangalasa yekha. Sanafune kukhala wozindikira yekha, sanafune kuti azikwezedwa monga Yohane mbatizi, anazichepesa kuti Yesu mwa iye akwezeke.

Nthawi zonse timakonda kuzilabadira tokha pakuganiza za ife tokha, tikuzipatula tonse kwa Mulungu. Nthawi zonse timapanga zisankho zokondwersa tokha; kuposa monga momwe tiriri, tikuzipatula tokha kwa Mulungu wathu. Nthawi zonse tikamaweluza anzathu timayesa kuti ndife apamwamba kuposa ena; tikuzipatula tokha ndi Mulungu wathu. Mulungu anati undikonde ndi mtima wako wonse. Iwe yense ukonde Mulungu ndi zinthu zonse zimene ziri zofunika kwa iwe zikonde ine ndikutumikila ine upezeke mwa Yesu ndi chizindikiro chako chonse. Undikonde ndi moyo wako wonse, upeze chizindikiro chako mwa Yesu ndi mwazi wake; zida zonse uli nazo zikuthandize kutumikira ine. Palibe mwini wa zinthu zonsezi ndi Mulungu basi. Tisanayade chifukwa cha zomwe Mulungu wachita ndi zake, ndipo ndizaiye yekha. Pamene timanga nyumba ndi manja athu tikabwera kunyumba imeneyi tisayende ndikuti, ee! Ntchito yabwino ndayichita; kapena kuti ndamanga nyumba yabwino; ndamanga ndi manja anga, ndagwira ntchito yabwino pokuva ana anga tisazipatse mphamvu tokha.

Moyo wathu uli wa Yesu ndi atate Mulungu akuti undikonde ndi mtima wako wonse ndi moyo wako wonse.

Malingaliro Athu Onse

Ndinafunsa atate tanthauzo la zimenezi, ndifuna iwe undikonde ndi maganizo ako onse. Nthawi zina zinthu izi zimasokoneza. Koma chinthu chimodzi anandionetsa chokhuza kukonda iye ndimaganizo wonse maganizo amane amabwera aziyimilira chisankho chimene ndimapanga. Ngati ndimkonda iye ndi malingaliro anga onse, ndiye pafunika ndizipanga

chisankho pa lingaliro lililonse lobwera kwa ine. Mawu amati, mwa Paulo mtumwi tirimange lingaliro lililonse. Tizilisusa lingaliro lililonse loyipa lomwe lichite chilungamo.

Mulungu amati chiri chonse chabwino chokoma, chiri chonse choyera, choyenera matamando, ganizani za zinthu zimenezi. Paulo amati, timasinthika pamene takonza malingaliro athu.

Aroma 8 amati malingaliro amene amatsogozedwa ndi mzimu wa Mulungu ali moyo Mtendere.

Kodi ena mwa inu mumakhalapo ndi mkwiyo wam'maganizo? Kapena lingaliro la Nsanje? Kapena la ukali? Kapena la chilakolako? Kapena la kunyada? Awa ndi malingaliro amene amzionetsela okha mwa iwe. Zili ngati munthu wa chichepela walowa m'malingaliro anu ndikuti, ndifuna ndikuonetseni kulingalira.

Mphamvu Zathu Zonse

Tonsefe tiri ndi zisankho zathu, tsiku lililonse, tizasankha kapena kuti maonekedwe athu apita kapena ayi pamene timkonda Mulungu ndi mtima wathu wonse. Tizasankha zimene moyo wathu watilora kuchita kapena ayi. Moyu wanga wandilora kupeza chizindikiro changa mu zinthu zina, kupatula mwa Yesu. Paulo anati, ndapachikidwa ndi Yesu akhala wa moyo mwa ine. Paulo anaconda Mulungu ndi moyo wake wonse. Chizindikiro chake chinali, mwazi wa Yesu basi.

Anathandauza Yesu basi osati chinanso. Ngati timakonda Yesu ndi moyo wathu wonse, tizalora mawu a Mulungu ndi malingaliro ake m'maganizo athu.

Sitizalora, kuphingika, kapena chilakolako kapena mantha ayi tizawachotsa m'malingaliro athu. Sitizalora malangizo a mkwiyo, kapena kusakhululuka, kapena Nsanje, kutilamulira ife tizachotsa m'malingaliro athu - sitizakhala ngati anthu a chikunja m'malingaliro koma anthu osinthika ndi otsimikika.

Tizakonda Mulungu ndi malingaliro athu onse. Tizaganiza za iye yekha basi.

Atate amandionetsa kuti mphamvu zathu zimatengera zinthu zambiri. Tikamkonda ndi mphamvu zathu zonse ndiye aziwe kuti nthawi yathu ili ya kwa iye. Nkhani yathu ili gawo la mphamvu yathu timulore Yesu, chikondi cha moyo wathu atiphunzitse m'mene tingapelekelele nthawi yathu kwa iye. Sitizalowa zinthu zoononga mphamvu yathu kutiononga ife, tizalora chikondi cha Mulungu pasi kuyenda mmoyo wathu, chakudya chathu chikhale gawo la mphamvu yathu.

Mfumu Davide mtundu wa Yesu, Ambuye akutionetsa chinthu china chofunika pankhani yakukonda Mulungu ndi mphamvu zathu zonse. Anthu ake akhondo anayenera kuziyiwala pamene iwo anali kumenya nkondo (1 Samueli 21:5)

Kuti tichite zazikulu za Mulungu zitengela mmene timagwiritsila ntchito mphamvu zathu. Tikagwiritsa ntchito mphamvu zathu pa china chilichonse, ndikunena kuti ndatopa sundingatumikire Mulungu, pamenepo ndiye kuti sitikonda Mulungu. Tizipanga chisankho chimene chingatipatse mphamvu zotumikira Mulungu mu nyengo zonse.

Ndalama zathu ziri gawo la mphamvu zathu. Ndalama zimachokera ku ntchito ya manja athu. Gawo la chisankho chimene timapanga pogwiritsa ntchito ndalama timatengera mphamvu zathu. Mtumwi Paulo anati, pamene iye anayenda mzinda ndi mzinda dziko ndi dziko. Anati, chifukwa ndasintha moyo wanu ndakupatsani choonadi chauzimu; ndiri ndi ufulu kukuuzani kuti mundipatse ndalama pa zonzezi.

Munkhozanso kudnipatsa mkate, koma iye anati, iyayi, ndikupatsani chisanzo cha momwe ndimagwirira ntchito ndi manja anga; usana ndi usiku kuti ndikhale wakuthekera kukupatsani ngakhale moyo wanu ndifuna chifukwa cha zinthu za uzimu. Ndakuphunzitsani, sindifuna kukuuzani, kapena zovala zanu, ingakhaleenso ndalama. Ndinena njira ya momwe ndingachitire. Ambuye wati, kupatsa kumadaritsa kuposa kupeleka; kotero ndizeza ntchito ya momwe ndingachitire nanu.

Paulo anati azera njira imene angathandizike nayo kuti atumikire Mulungu.

Mawu akuti tizipeleke matupi athu ngati nsembe ya moyo, ndi gawo la thupi lathu ngati zida za chilungamo. Paulo ndi atumwi ena a Mulungu anapachika matupi awo chifukwa cha kusagona tulo ndi kutopa.

Amapachika thupi lake pena akakhala ndi njala, kapena kulumidwa ndi zigawenga.

Pamene amaenyedwa nakhala tayile wakufa mu mzinda, chifukwa chakuti anaconda Mulungu ndi mphamvu zake zonse. Analalikilabe mawu osatopa ingakhale anaganiza kuti iye wafa. Petro ndi Yohane anali ndi mabala a zowawa zomwe anamva chifukwa chotumikira Yesu. Analalikirabe za nkhani ya bwino ya Yesu Khristu.

Stefano, Yakobo, Yohane mbatizi – anazipeleka kwa anthu potumikira Yesu ndi mphamvu zawo zonse. Ifenso tisakonde moyo wathu okha koma Mulungu, ngakhale mpaka imfa itipeze tikutumikira Yesu, tiyeni tidalire Yesu nthawi zonse.

Kulowetsa Kwa Kuya

Nditamfunsa Mulungu za ichi kuti chitanthauzanji? Ndinadabwa yankho lomwe iye anandipatsa akundifuna kuti ndimukonde iye ndi mtima wanga wonse. Chifukwa iye ndi Mulungu wa Nsanje afuna ndimukonde ndi moyo wanga wonse, chifukwa iye ndiwa sanje. Afuna ndimukonde ndi malingaliro anga onse. Ndikalimbana nazo zimenezi ndikuona kuti moyo wanga ukuyandikira ku zimenezi, ndiona kuti iye akunditengela kw aYesu mozama. Akundipanga ine wanzeru, ndiwokonda komanso womasuka. Akhonza kupangitsa mitsinje ya madzi kuchoka mwa ine monga Yesu analonjeza, akhonza kuzika zinthu zodabwitsa mwa ine ndi mphamvu yake, akhoza kuyika zida za chilungamo kudzanja langa la mazere ndi lamanja.

Eliya munthu ngati ife analamula mitambo isavumbitse mvula, amalamulanso kuti mvula igwe ndipo inagwa. Mawu akuti, Eliya anali ngati ife, palibe chovuta ndi ife ngati tiri ndi Yesu, ndikukonda Mulungu ndi moyo wathu mtima wathu ndi mphamvu zathu zonse. Anthu ambiri sakonda Mulungu ndi chiri chonse chawo. Mukondeni Mulungu ndi mtima, moyo ndi mphamvu zanu zonse.

Ndikuthandizana Wina Ndi Mzake

Gawo liomodzi lakukonda iye limachita chita pamene ife tikonda anzathu amene tikhala nawo limodzi. Kuwakonda ndi zonse zomwe tiri nazo

mtima wathu wonse, moyo wathu wonse, komanso mphamvu zathu – zonse. Akaona wina pafupi ndi iwe akhoza kukhala mbale kapena mlongo, sakonda Mulungu ndi mtima wawo, moyo wawo, kapena mphamvu zawo, Mulungu akuti tiwathandize kuti azitero.

Akuzitora okha komanso panthawi yomweyo abela Mulungu, tikatero, mpingo uzakhala chinthu chaku

Koma zimenezi zimayenda ndi ife ngati munthu m’modzi. Mawu akuti mkondeni iye ndi mtima, moyo komanso ndi mphamvu zanu zonse.

Ichi chinali chakwa inepakatipaine ndi Mulungu, koma ngati ndizothandiza kwa inu, pamenepo ndingati ndinali nawo mwayi woti tikambirane.

Mapelekedwe A Ndalama Mu Ufumu Wa Mulungu

October 6, 1999 Lilongwe, Malawi Africa

Ku mpingo umene ine ndimakhala kulibe aliyense amene amalipidwa ndalama palibe aliyense amene amatenga ndalama kwa iwo wokha palibenso amene amaphunzitsa kuti apeze ndalama. Koma aliyense ali otanganidwa kupereka monga takhaliramo sitiyendetsa nsengwa koma koma wina aliyense amathandizidwa ku nchito ya Mulungu mu chuma. Pali anthu ambiri amene amapatsidwa udindo mu nyumba mwawo mwa nseri umene abale ndi alongo amapereka pochita zimenezi timafuna kuti dzanja lamanja lisadziwe zimene la manzere likuchita. Sapita kutsogolo kukapereka ndi kuona anthu onse koma amapereka kuchokera pa mtima pawo.

Pali zinthu zambiri zimene anthu ayenera kupereka. Abale ena amaika mu enevolope ndi kujlemba kuseri kuti zigwire nchito yoti. Akhoza kuti kwa “osauka” kuti amene ali osowa pakati pathu kapena mu malo amene timakhalamo angalembeenso “zosindikizira mabuku” Monga mwa mabuku amene mwalandorawa ambiri oyera mtima anapereka zopeza zawo chifukwa linali pemphero lawo ndi mtima kugawa choonadi chimene chinali chopambana kwa iwo. Ena angathe kupereka kwa mbale amene akutumikira Ambuye kwambiri, mwina ali ndi ulendo wopita kwina. Sali pa ntchito yomwe amagwira koma chifukwa akufuna kuti akakhale ndi okhulupilira ena kwina amapereka mbali ya zopereka zawo pa chifukwa chimenechi.

Kulemba kuseri kwa enivolopu kumathandiza kulumikiza miyoyo yawo pa zimene zikuchitika. Osangopereka ndalama mosawonetsetsa mu nsengwa ai. Koma ndalamazo zikuimira nchito ya Mulungu. Pamenepo ayenera kulumikiza ntchito imene ili yofunika ku maganizo awo. Sangadziwe kuti sabata ino akapereka kwa ndani ndiye angaika kuti atsogoleri pali zambiri zochitika ndithu.

Mu zaka zoyambilira Chikhristu nthawi zina anthu amaguritsa nyumba ndi kuika ndalama pa mapazi a tumwi ndi kutumizidwa monga kufunikira

ndiye nthawi zina zimatero. Kwa nthawi amapereka kwa zinthu zodziwika bwino chifukwa palibe amene ali kuona zingakhaleenso ndi ulesi chifukwa dzanja la manzere silikuona la manja. Mungakhale aulesi mukupereka kwanu. Aliyense ayenera kukhala osamala kuti asalore izi kutero. Anthu ambiri ku Amerika amalandira pa ssabata iliyonse uku ndi chabwino kukumbutsa kuti atenga ndalama ku ntchito ya Mulungu. Kodi zayankha funso lanu? Palinso lina? Kodi ndasiya zina zimene zikanathandiza.

Nanga Za Chakhumi?

Chiphunzitso cha chakhumi sichili mu Chipangano chatsopano ngati mukufuna kupereka chakhumi ndiye kuti muyanera kupereka nsembe ya nyama. Ndi chiphunzitso cha Chipangano Chakale. Chipangano Chakalelinali kumvera pa zimene Mulungu ananena kwa anthu ake mu Chipangano Chakale. Chakhumi sichilinso mbali ya nsembe za nyama kapena munthu woyera kapwina wa nsembe kapena kupembedza kwa kuasinsi zinali mbali ya phangano la mwazi wa Yesu, Sali chakhumi mulibenso. Palibe kupereka chakhumi mu mgwilizano watsopano. Anthu amapeza ndalama kwa nkhusa za Mulungu pazogula (zomanga za chipembedzo) ndikulipira malipiro kwa anthu. Potenga malamulo akale ndi malembo kuti anthu a Mulungu apereke, motero anthuomwewa sanenanso za loweruka monga (sabata) kupembedza ku Yerusalemu mkansinsi) kapenanso nsembe za nyama zimene zili mu gawo limeneli. Ndi kusakhulupilika kuchotsa zinthu zina ndi kusakhulupilika kuchotsa zinthu zina ndi kulowetsa zina ndi kuti zinthu zidzikhala motero.

Paulo aanaphunzitsa ndithu kuti tinafa ndi machismo athu ndi mwazi wa Yesu ndi osakwanira kwa ife ngati tikhale mu pangano la kuumbala ndi kusunga sabata ndi kupereka Chakhumi. Palibe gawo lina kupita kwa mbusa mu Baibolo. Iyi sinjira ya Mulungu.

Mu pagano ili Mulungu amafuna ndipo alikufuna kuchokera mu mtima ndi kuti zichokera mu Mzimu. Yesu anati ngati mungapambane chilungamo cha Afarisi simungathe kulowa mu ufumu. Mu pagano limeneli liyenera kukhala mu UBWENZI mu moyo, chikondi chalero ndi Messiah. Kupereka kwathu mu pangano la tsopanoli liyenera kukhala kudzipereka monga mwa kulamula kwake ndi kumvera kwa Mzimu wa Mulungu tsiku ndi tsiku.

Pamene Yesu anaima pa kasinsi mkati anaona mzimayi amane anapereka kwambirimu choperekera ndalama sizidali zochuluka ai monga mwa myezo. Yesu sanati anapereka gawo khumi. Sanaperekanso chakhumi koma anapereka anapereka ndalama zake zogulira chakudya. Mulungu anali opambana kwa iye koposa chakudya. Anakonda Mulungu wake ndi mtima wake wonse moyo, Maganizo ndi mphamvu zake zonse. Sanali fkufuna njira yoperekera mbali ya gawo. Amafuna kupereka Mphatso imene inalipo ndipo Yesu anati Taonani mzimayi uyu Angelo ali kuimba nthungululu ndi kuomba mmanja kwa iye chifukwa sanaganize za chakhumi anapereka mtima wake wonse, maganizo, moyo ndi mphamvu zake zonse. Uwu ndi uthenga wa Chipangano Chatsopano ndipo Chipangano chakale ndi chofooka monga mmene chilili.

Popanda Cholowa

Pamene Paulo amalemba kwa mipingo anati, *“sitifuna phindu ku mawu a Mulungu.”* Paulo samaona ku Mphatso yake ngati chinthu choti amangire anthu osati kuti apeze ndalama kuchokera kwa anthu. Iye anayetsa kupereka monga tanena kale ena anazipereka kuti mabukhu amene tabwera nawo asindikizidwe. Sitikugulitsa mabukhuwa tikupereka mabukhuwa kwa inu ndi kwa ena onse. Ziphunzitso za mabukhuwa ndi a Yesu osati Iye Yesu anagawa zinthu zimenezi kwa ife mwaulere ndiye ndithu tifunanso kugawa kwa inu ulere

Ndikujyembekeza kuti sipakhala wina ogulitsa limodzi la mabakhu kwa aliyense. Ndi Mphatso imene Yesu wapereka kwa inu, ngati ndi chiphunzitso ngati ndi nzeru ngati ndi chidziwitso ngati ndi kuimba kapena kusewera ndi choimbira ngati ndi kuthekera kwa kulankhula bwino ndi zinthu zimene zaikidwa ndi Ambuye kuti muzisalire ndipomphatso imeneyi ndi ya Yesu koma waizeza kwa inu kuti zipindulire anthu ena tsiku lina Yesu analankhula ndi Afarisi ngati mungapemphere kuti ena akuyamikireni ndiye kuti mwalandiratu phindu lake izinso ndi zoonza mu nkhani ya ndalama. Ngati mungaphunzitse kapena kuelmba nyimbo kuti ena akulipireni ndiye kuti ndalama imeneyo ndiye malipiro anu. Koma ngati mukufuna kupereka mwaufulu pa zimene Yesu wapereka kwa inu ndipo malipiro ndi akulu. Madalitso ake ndi ochuluka mu miyoyo yokuzungulirani ndipo uzdakhala kulemekeza Mulungu.

Mu zochitika zinanso, aliyense anachita chiganizo kwa Mulungu mu sabata inailiyonse monga angakhalire opereka mmene angaperekere zinthu zawo pakati pa iwo ndi Mulungu amapanga cholinga chifukwa choti amamukonda ndi mtima wawo wonse. Amachita chisankho ndiye amaganiza kuti angapereke ndalama zimenezo. Pali okhala nawo pafupi amane abale oyer mtima amakhala nawo pamodzi. Timaika box kumodzi kwa nyumba zotere ndiye abale amene amakhala mu zinyumbazi za kumeneko amapita mwakachete ndiye amapempha Mulungu kuti alandire Mphatso yawo. Analemba kalata ndi Mphatso ndi nchito yake imene yaperekedwera ndiye amaika mu choikira ndi kuchoka.

Ndiye tili ndi abale awiri kapena atatu amene amapita ku zinyumba zimenezo (midzi yaing'ononidiye amatenga ndalama kuika malo amodzi ndiye abale osankhidwawa, okhulupilika amagwira ntchito pamodzi amatenga ndalama zimene zalembedwa kwa osauka ndi kutumiza kwa osauka mokhala mwathu. Ndalama zimene zaikidwa kusindikiza mabuku odzafika ndalama zonse pamalo amodzi ndi kupereka kwa iwo amene amasindikiza, ngati pali mbale kapena mlongo amene moyo wawo easintha mabanja awo asintha pa Mphatso ya anthuwo angathenso kulemba dzina angathenso kulemba dzina la munthuyo ndiye abale okhulupilidwa amagwira ntchito pamodzi amapereka kwa iwo amene maina awo analembedwa pa envolopu kuti alandire moyenera. Monga Paulo abale enawo ndi alongo oyenera kupanga ma tenti kapena nchito ina chifukwa Paulo anakhuzidwa ndi miyoyo ya anthu ku Filipi ndi Atosolonika, amatumizira Mphatso pa ntchito kumeneko ndiponso amawasamira ena osowa ndi Mphatso. Amathandizanso abale ena monga Timoteyo ndi Taitasi ndiye kuti sanali kumanga tenti nthawi ndi nthawi mu kalata yak u Afilipi. Paulo anati timalandira nthawi zina ai. Nthawi zina analuka matenti nthawi zina ai. Ngati Mulungu amawathandiza pa zosowa zawo mu njira ina ndiye kuti zinali zabwino ngati ai. Anali kumanga matenti ndi kuthandizanso anthu ena. Popanda vuto choncho abale amene amatolore ndalama anagawa kwa amene dzina lake lalembedwa pa envolopu ndiye satenga kanthu paiwo wokha kodi zikumveka zimenezi.

Pamene wina akupereka ndalama kwa mzake amene wasintha moyo palibe amene amati alandire ndalama chifukwa kuti moyo wake wasinthika. Palibe amene amati ndilandire ndalama. Aliyense amafuna kutumikira

Yesu pa Mphatso ili yonse ali nayo. Aliyense osati abusa ndi anthu ena onse. Aliyense mphatsozina ndi zothandiza. Pamene Mphatso zimenezi zikuthandiza inu timafuna kuthandiza mwaulere kuti Mphatso ithandize enachoncho nthawi zina zimachitika koma osati chifukwa wina akuchita malonda mau a Mulungu ku phindu. Cholinga chawo ndi kuthandiza ndi kutumikira sakufuna kupeza ndalama susunthuka kwa iwo kumanga kwa nthawi zaka zisanu kapenanso amasulidwa kwa nthawi amatumikira Ambuye ndi moyo wawo nthawi zonse. Izi ndi zosiyana mmene dziko la chipembedzo limachitira. Anthu amaona mau a Mulungu monga ntchiyu. Sintchito monga umisiri wa matabwa zimenezi mulibe mu Baibolo.

Ndi Bwino Kupereka

Tiwonjezenso Yesu amati tikudalitsika kupereka koposa kulandira ndi kwabwino kulandira koma kwabwino kupereka koma sikwabwino kufuna kupatsidwa osati ana anga akandiuze abambo, abambo tipatseni kanthu ine ndi kumapitiriza ndikulira. Chimene ndingapereke ndi monyinyirika koma ndikuona ana anga ali kugawa ndi ena ndi kukonda anthu ena . Ndidzakhuzidwa ndi kumudodometsa ndi Mphatso. Izi ndi zoonadi mu banja la Yesu pasaooneke wina amene ali kuumiliza kuti alandire ndalama palibe amene anene mau anati, tili ndi zonse mofanana muyenera kundipatsa ndalama wina asadziyerekeze kunena kuti malemba amati, “ngati uli ndi Malaya awiri pereka limodzi kwa mbale, muli ndi Malaya awiri linalo ndi langa kumeneku ndi kuchimwira kumeneko ndiye kudzikonda choncho ngati wina ali kuumiliza ndalama kapena kena kali konse mpingo usamupatse kwambino kuti awawitsidwe mtima ngati zoonadi kuti ofunikadi kuthandizidwa ndipo abale aonadi kufunika ndi mu chikondi ndi kufnika kugwira nchito ya Yesu amapereka ndi zabwino ndipo ndi zobvamerereka.

Aliyense Amagwirira Nchito Mulungu Kwa Nthawi Yonse

Pamene Paulo anayenda kuchokera mu mkzinda ndi mdziko kuphunzitsa ena, Paulo sananene inde ndine mtumwi wa Mulungu wapamvandu! Sindingadzitsitse ndekha kupanga matenti. Ndine mtumwi wa Mulungu

wamoyo. Paulo anali kupanga matenti pamene amafuna ndalama ngati Mulungu amampatsa mu njira ina zinali bwino koma sanali odandaula kuti ali kumanga matenti. Ngati amamanga matenti ndiye kuti amakuna ndi anthu amenenso amachita chomwecho amene amafuna nsaru zopangira matenti anthu amene amadzagula ,matenti amene amawamanga ndi zimene iye amachita. Iye samasamala kuti anthu apeza ku msika kapenanso musunagogi, moyo wake wonse unali kukonda Mulungu ndi anthu ndi kwa anthu onse mu nthawi ina iliyonse ngati anali ku ndende amayenera kumusandutsa wa ndende ngati anali pa maso a mfumu kudikira mulandu amayesa kusandutsa mfumu ngati akupanga tenti amayesa kusandulitsa omugulawo mmene amapezera moyo wake sizinasinthe kanthu kali konse. Ngati Mulungu apereka zosowa kuchokera kwa abale ndi alongo amene akonda Iye ndipo ali oyamika ndipo anali omasulidwa kumanga tenti kwa kanthawi ndiye anali ndi mpata woyenda nkdi sailasi ndi abale ena kupita ku mizinda ina ngati analibe ndalama monga mmene ananenera mu kalata ya Afilipi monga amachitira. Amapanga matenti kwa kanthawi popanda bvuto.

Miyambo ya anthu zatiphunzitsa ife zoipa pa kunena kuti ndife azitumiki a Mulungu. Paulo anali wamtumiki wa mphamvu koposa anthu ang'ono otenga ndalama kapena osatenga ndalama. Paulo amagwira nchito molimbika ndi manja ake usiku nsi usana ndi kulipira chakudya changa pamene ndinali ndi inu. Mukandipezera chakudya koma ndinalipira ndekha ndimagwira nchito molimbika ndimanja potero kuti tikwaniritse zosowa zanga ndi ena.

Ngati ndizoono mu Mphatso yaikulu monga Paulo bwanji Mphatso zazing'ono zinaganiza kuti ndizosafunika kuti asamagwire nchito ndi manja awo? Ngati Mulungu angatithandize mu njira zina ndabwino koma tisayembekezere kapena kuwumiliza. Ngati anthu a Mulungu ali ndi mtima opereka ndi kutimasula kuti tisamange matenti ndi zabwino. Ngati titumikire tiyenera kupanga matenti ndiye tidzapanga matenti ndi kutumiza kwa zosowa za anthu ena.

Choncho zimenezi ndi zimene takhala tikuchita kwa zaka khumi ndi zisanu(15) kwa iwo ambiri anali a Zimbusa kapenaso atsogoleri anasiya malipilo awo ndi zolandira zawo ndipo Mulungu wakhala okhulupilika ndipo palibe mwayiwo ali ndi njala ndipo ali kutumikira Mulungu nthawi

zonse. Oyera mtima onse ndi ana alikutumikira Mulungu nthawi zonse, satumikira Mulungu polandira ndalama amatumikira chifukwa cha chikondi ndipo Mulungu amawapatsa njira zosiyanasiyana. Ichi ndiye choonadi changwiro koma ndichochititsa mantha nthawi zina kuti tisiye miyambo ya anthu. Pamene ndalama sizikhalanso mumatumba athu palibe amene anatumikira Ambuye munjira imeneyi, Mulungu ndikulephera. Ambuye ndiokhulupilika ndipo amasamala akhwangwala ake, amasamalanso mbalame zamulengalenga, amasamalanso iwo amene akonda iye. Palibe opambana anzawo muchikristu.

Palibe muchikristu pamene anthu amagulitsa mphatso zawo, pamene ena alibiletu mphatso. Palibe amene agulitsa mphatso yake mumpingo ndipo Mulungu amaona aliyese monga kufunika kwake, ndipo Mulungu ndiye amafuna kuti kuchitike ndi zofunika zathu. Ndiye atumiki ake Amulungu nthawi zonse amatumikira kaya ndi kusika, kapena ku ndende, kunyumba kwathu zonsezi ndi choonadi chofunikira. Tiyenera kugwedeza mtengo wa miyambo ya anthu ndikuyigwetsa pansu. Mulungu ndiokhulupilika ndipo azatiteteza ife ngati tichita chomwecho.

Mwachitsanzo ambale ena ndi alongo anafunitsitsa kuti ife tibwere kuno sikuti tidangoganiza choncho kapena kuti ndife odziwika, kotero kuti tingapite kwina kulikonse. Sitili monga choncho, ndife akapolo chabe monganso inunso muli. Kunali kufuna kwao osati kwathu aziperekanso kulipila zithu zina, pamene ife tili kuno.

Sitinawafuse kuti atero . Anthu amulungu amamva Mulungu ndikuganiza pamodzi kuti tibwere, ndimmene zinakhalira.

Mayeso amene Yesu anawapeza pakati mkachisi ndi amene ali ofanafana ndiamene ifenso nthawi zina timakhala nawo, sichoncho?

Kodi tikhulupilira zimenezi?

Funso (La Msiska) Pamene tafuna kupereka uthenga wa mfumu ndi umfumu wake ndi abale amene ali kuchipembedzo pokhudzana ndi ndalama zimene iwo amalandira tingawauze chiyani pokhudzana ndi ndalama zimene amalandira? pamene iwo adalira ndalamazo pa moyo wawo.

Ngati munthu afuna kukhala kuchipembedzo chifukwa cha ndalama Mulungu adzamuweruza kwambiri. Ngati munthu akana choonadi cha Mulungu chifukwa cha ndalama, ndiye kuti ndiwopembedza wa Satana. Tikulankhulazi siza ndalama! *Izi ndi za Mulungu, amene ali wamkulu koposa ndalama!* Tiyenera kunkhulupilira Mulungu ndikumumvera iye muzowawa zonse. Ngati ndizowawa za m'banja kaya ndi nyumba, kaya ndi ntchito, kaya ndalama zathu zonse-zimenezi ndizithu za Yesu zomuyenera muzilizonse zokumana nazo.

Petulo ndi Yohane adati, "siliva ndi golide NDILIBE. Koma ndili ndi Yesu ameneyo ndikupatsa iwe". Ngati chipembedzo chimwaza ndalama kwa wanthu ndiye kudalira kwawo, ndipo anthu amenewo akayamba kumvera Yesu polandira zowawa zilizonse, chithu chimodzi kapena ziwiri zidzachitika choyamba kuchitika, ndiye choonadi cha Mulungu chidzabwera chipembedzocho ndikusintha chipembedzo chonsecho. Anthu adzayamba kupeleka ndalama chifukwa miyoyo yawo yasinthika. Chinanso chidzachitika kuti chipembedzocho chidzasiya kupeleka ndalama. Ndipo ngati asiya kupeleka ndalama... Ndiye kuti *"ZIDZAKHALA CHONCHO!" Ambuye adzapereka kwa omvera ndiokhulupilika.*

Kodi timankhulupilira kuti Mulungu ali ndi ng'ombe m'mapiri? Kodi timakhulupilira kuti tikafunsa iye m'dzina la Yesu adzatipatsa? Kodi timankhulupilira kuti amatikonda kwambiri koposa khungumbwi ndi maluwa ammunda? Kodi chingakhale kuti ndi chipembedzo chabe chofuna kupeza zithu mwa ife tokha? Ngati mutsata njira ya Mulungu potsata ndalama, kapena ngati munyengelera ndikusiya choonadi cha Mulungu chifukwa cha ndalama ndiye ndikuuzani chithu chimodzi monga Paulo adati kwa Simoni wa nyanga. "Iwe ndi ndalama yako utaike nayo ku Jehena" Tisakhudzidwe ndi ndalama. Tinkhulupilire Mulungu ndikumvera Mulungu muzowawa zili zonse iye ndiye atate odabwitsa amene akonda kupeleka mphatso zabwino kwa ana ake.

Ganizirani zimenezi.....

Pamene Ethiopia lidali dziko la chikristu ndipo anthu ndikumaopa Mulungu, Ethiopia adatchedwa mkate mundengu la Afrika.

Chabwino ndi Mulungu amene amamvubwitsa mvula, kuti mela ukule ndi ziweto kusangalala ndiponso dziko kutukuka. Pamene Ethiopia anakhala dziko la chisilamu ndipo chihristu chinapeputsidwa, Mulungu anaweruza dzikolo ndipo mvula inasiya kugwa. Ethiopia lero ndichipululu osati mkate odzadza.

Siyani ndi kuganizira zimenezi chifukwa chimene ndikulankhulachi ndi chimene chimabwezeletsa choona mmbuyo. Ngati tidzamanga nyumba ya Mulungu osati mmamangidwe athu ndipo ngati tidzapeleka tokha poteteza chuma chathu ndiye kuti Mulungu adzakulitsa mbeu yathu. Adzagwetsa mvula, ndipo ma bizinezi athu adzatukuka, ndipo adzapeza njira yotisamala pa zofuna zathu

Ngati Njira ina tiziteteza tokha ndi kunyengelera pakusamvera choonadichi chifukwa cha mantha pa zimene zingatigwere, ndiye Mulungu adzatilanga. Kotero kuti matumba athu adzakhala obowoka . Ndalama zomwe timaganizira zizizakhalanso motero. Mbeu zomwe tizabzala mmunda zizakula moyenera koma ngati tikulupilira Mulungu adzatisamala ife tonse choncho ngati sitimvera adzatiweluzwa ife monga anena(Haggai Chaputala Choyamba)

Ndiliti Mulungu adzakhala ndi athu amene amukhulupilira iye kotheratu ndi kumvera iye mu zowawa zirizonse? Kodi mudzakhala muli inuyo? Ngati sichoncho mudzaola . Mudzakhala opambana mu ULEMELERO WA MULUNGU

Ambuye Mulungu wamphamvu , choonde mvetselani pemphero lathu tsopano, Tikupemphani inu tsopano kuti mutsegule ku mwamba. Choonde pitilizani kuthila bvumbulutso kwa abale ndi alongo okhulupilikawa, pitilizani kuthila mafuta a chikonweleru kwa iwo amene amvera. Pitilizani kumanga mpingo wanu ndi nzeru za kuya Chikondi ndi kudzipeleka kwaiwo onvera inu mudipo lilonse tikupemphaninso Atate Mulungu monga mwa malonjezo anu mubuku la Detolonome kuti mudzabweretsa matembelero ndi ma weluzo kwa iwo osamvera inu tikufunsaninso kuti mukhale Atate athu ngati tikonda ndi kumvera inu tikufunsani kuti mukhale oweruza ngati sitimvera inu tikudziwa kuti simufuna

kubweletsa zoipa koma tidziwa kuti tiyenera kumva zowawa pokonzaso mizimu yathu tikupemphaninso kuti mukonze mitima youmitsa ngati tili nayo tikupemphaninso kuti mutikumbatire ndi kuthandiza kufowoka kwathu. Chonde chotsani kuukila kwathu ndipo mutithandize pa kufowoka kwathu . Tikukuitanani tambasulani nkono wanu kuti muchite zonse munjira ya Umulungu. Tidziwa kuti inu mulipo wamoyo ndi waulemelero. Awa simasewera chabe sikuti tikungokusankhani inu kukhala Mulungu wathu.

INU NDINU MULUNGU, Ndipo tiyenera kugwadira inu. Ndife opusa ndi ofowoka nthawi zonse, koma tikuitanani kuti tikhale abambo ndi amayi a Mulungu, onongani kuwukira kwathu. Tipeleka ullemero kwainu Oyamba ndi Mlengi okonda miyoyo yathu ndi mmisiri wa mpingo wanu, lilemekezeke dzina lanu AMEN

Kufunduka Kwa Gulugufe.

October 1999, Africa.

Funso: Pamene tikugawana ndi anthu choonadi cha Yesu ndipo anthu akufuna kulapa ndi kufuna kutuluka mu zipembedzo zawo, Tingawauze chiani?

Ngakhale kuti anthu akufuna kuchoka muzipembedzo, ndizabwino kusakana ngati kungatheke chifukwa chache ndi ichi; ngati atadziwa, kapena apeza choonadi chi cha Mulungu monga kulapa machimo kwa wina ndimn'zake, kutengelana zo thobwetsa, kuchengetana wina ndi mnzake tsiku ndi tsiku, ndi kuchotsa chotupitsa pakati pa abale. (Choonadi ichi chakhala chili mu Baibulo kwa nthawi zonse, koma chaiwalidwa kapena kuiwalidwa kapenanso kutchutsidwa) ndiye ayenera kugawa zinthu izi kwaanzawo apafupi. Tiyenera kukankha anthu kuti atenge choonadi ichi chimene aona kuchokera kwa Mulungu ndi kugawiranso kwa anthu ena amuchipembedzo.

Ali ndi abwenzi ndi apabanja amene ali m'bali ya chipembedzo. baibulo limati amene wapatsidwa kukhulupilidwa ayenera kusonyeza kukhulupirika pa chinthucho. Ngati munthu amene takumana nayeyo ali ndi mphatso yochokera kwa Mulungu kudzera mu mau a Mulungu, atenera kukhala okhulupirika ndi omvera ndi mgwilizano umene ulipo kale pamene anthu ali omvera ndi okhulupirika ndi mgwirizano umene ulipo, ndiye kuti zinthu chimodzai kapena ziwiri zidzachitika. Miyoyo ya ambiri kapena monga Yeremiay, munthu amene akuyesa mukukhala mu choonadi cha Mulungu adzachotsedwanso nawo pamodzi, ndi kuthamangitsidwa kuchokera mu chipembedzo.

Koma amene walapa potulukira kunjira kwa chisteko sakukhala okhulupirika ndi choonadi chimene Mulungu wapatsa iwo. Ngati muli mu Hotela ndikuthawa fugo la usti ndikuona kuti muli moto ngati mungothawira kutulukira kumbuyo kwa chitseko mudzakhala ndi dzanja pa anthu amene afawo. Ngati wina wadziwa kuti chipembedzo chili kupsya usangowasiya kuti atulukire ku mbuyo ya chitseko. Timawaphunzitsa anthu kufuura pamwamba pa nyumba, "Dziwani njira za Mulungu!"

mvelani Mulungu! Ndili ndi uthenga wabwino - zilipo zambiri zimene angakhale tsopano sitinadziwe pa choonadichi! Tingamasulidwe kuchoka kudziwe pa choonadichi! Tingamasulidwe kuchoka kuchimo! Tingakhale anthu amodzi m'malo mwake kapena otayanatayana aliyense! Tingakhale mpingo woona umene makomo andende akufa sangathe kupambana. Choncho timawapempha anthu kuti akhalebe mu chipembedzo ndi kukhala okhulupirika ndi mabanja awo ndi abwenzi awo ndiye mirakulu idzaoneka kapena adzathamangitsidwa koma sitimalora kutuluka ku mbuyo kwa chitseko pamene fungo la moto lawoneka.

Ngati aliyense ndi omvera munjira imeneyi ndi kuitana wina ali yense kukhala okhulupirika mu njirayi, ndiye kuti siife amene akumanga mpingo wake. Sitikupeza anthu anthu amene amaganiza monga ife timaganizira. Tikufuna kuti wina ali yense amvere njira ya Mulungu. Kuti konse kumene ali ndipo pamene Yesu agwedeza mtengo zipatso zabwino zimagwa. Akhonza kukhala anthu khumi abwino mu chipembedzochi. Angakhalanse anthu zana limodzi mu chipembedzochi. Koma ngati wina athawira kukhomo la kunja ndi kusiya chipembedzo kachete chete, ndiye kuti pali anthu khumi kapena zana amene anakatha kusinthika miyoyo yawo ndipo sadzadziwa.

Ngati muli ndi khungwa lagulugube ndipo mutenga reza ndikutsegula mkati mwa Gulugufe, sadzauluka. Ndi ndondomeko yomenyera Gulugufe imene Gulugufe amakhala ndi mphamvu wowulukira!

Afunseni anthu amene ayamba kale kuwoona choonadi ichi cha Mulungu kukhala ndi kukhulupirika ndi anansi awo ndi mabanja awo asanyengelere ayi komanso kukhotera mu kusamvera. Afunseni kuti aime ndi kulimbika muchoonadi chimene apeza kuchokera kwa Mulungu. Ngati adzakhala okhulupirika, omvera, olimbika, ndi kulola kupeleka dipo posawelengera kukanidwa, ndipo adzakhala monga MBOZI imene ikusandulika Gulugufe ndi kuchoka mu chikhombe chake.

Anthu ambiri adzaphunzira njira ya Mulungu pakukanidwa kumene kwachitidwa ndi moyo wawo. Ndiye sitiba kukula kuchokera mudula poyera chikhungwa ndi kutenga Gulugufeyo. Timayetsetsa kuti njira yotulukira ipezeke - choncho kuti **AKHONZA KUWULUKA.**

Zochitika Mu Dziko La Chipembedzo

October 2, 1999, Salima, Malawi, Africa

Ndifuna kulankhula nanu kwa kanthawi yochePAYI za anthu a Mulungu amene anakhala zaka zikwi zitatuzo. Amenewa anali Aisrael, adali ndi kachisi ku Yerusalemu pa phiri lotchedwa Wazion. Linali nyumba yomangidwa. Idali yokutidwa ndi Golidi ndi kukutidwa ndi matabwa okongola. Nthawi zambiri pa chaka anthu amabwera kunyumbayi. Anali ndi masiku opatulika. Anali ndi nthawi yopuma imene ali kukumanako. Anali kupeleka nsembe kwa Mulungu. Anali kufuna kubwera pafupi ndi Mulungu. Ansembe anali kuthandiza anthu ku Kachisi. Ansembe anali kuthandiza anthu kufika pafupi ndi Mulungu, Ansembe amapeleka nsembe za nyama. Ansembe anali kupha nyama ndi kuwaza mwazi pa guwa kuti machimo a anthu akhululukidwe ndi kufika kwa Mulungu pafupi.

Izi inali zaka zikwi zitatuzo, tiyeni tilankhule za anthu alero. Tilankhule za Israel woona. Abale ndi alongo ngati munapereka moyo wanu kwa Yesu ndinu Israel woona wa Mulungu, Amen ngati munapeleka moyo wanu kwa Yesu. Ali mfumu yanu ndinu Israel wa Mulungu.

Ndinali kukhala pano ndipo ndinaona munthu alimkututsa, pamene ali kudutsa panali chithunzi kumbuyo kwake. Pamene munthuyo amayenda, chithizichonso chimayendapamene anakwezadzanjalake. Chithunzichoso chimakwezanso dzanja, chithunzicho chinali ndi miendo. Chithunzicho chinali ndi mutu. Kodi chithunzicho chinali munthu? Ai, chithunzicho sichinali cichinali cheni-cheni. Chimaoneka ngati munthu. Chimayenda monga munthu koma mafanizidwe a munthu. Abale ndi alongo ana a Mulungu mu zaka zikwi zitatuzo anali mthunzi wa ana a Mulungu. Lero tilankhule za chithunzi chimenechi.

Kale, kunali kasichi, lero tilibe kachisi omangidwa ndi manda. Lero inu ndinu kachisi wa Mulungu. Mulungu sakhalanso mu nyumba zomangidwa ndi manja. Lero, inu ndinu Kachisi wa Mulungu. Mulungu

sakhala munyumba. Yesu amakhala mu mitima ya amene anamusankha iye monga Mfumu. Simufunikanso kupita ku malo opatulika. Ngati muli woyera ndiye kuti ano ndi malo wopatulika. Simufunikanso kupita kwina kuti mupeze pafupi Mulungu mungadziwe MULungu mu mtima yanu. Ndinu Kachisi.

Abale ndi Alongo simufunikanso masiku apadera dera. Lero ndi tsiku la chipulumutso, LInena, “Lero musaumitse mitima yanu. Samalanani wina ndi mnzake tsiku ndi tsiku. Sitidikira tsiku la Mulungu, sitidikira nthawi yolambira. Masiku asanu pasabata ndi maora makumi awiri ndi anai pa tsiku tingakhale pafupi ndi Mulungu ndiye sitifunikanso kukhala ndi malo apadera kapena nthawi yapadera.

Nanga za ansembe? Ntchito yawo inali yoyandikitsa anthu kwa Mulungu. Tsopano tilibe chithunzi, tili ndi choonadi. Lero ansembe a Mulungu ndi INU. Ntchito yanu ndi kuziyandikitsa nokha kwa Mulungu mu mitima yanu ndi anthu ena pafupi ndi Mulungu. Poto simufunikanso munthu kubvala zobvala zapadera kapena kuzitcha ndi maina ena chifukwa mutha kukhala wansembe wa Mulungu.

Lero Ufumu wa Mulungu suli mu malo. Suli mu nthawi, suli mu nyimbo zapadera. Uli mwa anthu amene akhala mwa iye. Anthu amene angatumukire Yesu kasanu ndi kawiri pa Sabata, makumi awiri ndi anai pa tsiku. Anthu amene amakonda iye ndi mtima wawo wonse. Maganizo, umunthu ndi mphamvu zonse pamene Yesu anali kuyenda pa dziko lapansi pano, adalankhula ndi mzimayi. Adamfunsa funso; Tingalambire kuti Mulungu? Kodi ndi mphiri ili? Kapena linali? Yesu anayankha, “Osati malo ano” Ufumu wa Mulungu suli pano kapena uko “Ufumu wa Mulungu uli mwa inu.”

Opembedza otere amene Atate afuna kuti ampembedze iye mu mzimu ndi mchoonadi. Amen Anthu a Mulungu ndi amene amapembedza Mulungu kasanu ndi kawiri pa Sabata. Makumi awiri ndi anai patsiku pakukonda ndi miyoyo yawo palinso zambiri za kachisi. Munthu m’modzi sangakhale kachisi, Inde, Mulungu angakhale mu mtima wa munthu m’modzi. Koma ali yense ndi mwala omangidwa pamodzi ndi miyala ina kukhala kachisi. Tiyenera kufunana wina ndi mnzake. Ndingapembedza Mulungu motani tsiku lili lonse? Kolingana ndi mau a Mulungu pokhapo nditalimbikitsidwa

kuchokera kwa abale ndi alongo tsiku ndi tsiku. Mtima wanga udzauma kwa Mulungu moyo wanga udzadzaza ndi chimo. Ndidzaumilitsidwa ndi chimo. Ndiyenera kupeza abale ndi alongo kundilimbikitsa ndi kutonthoza ine, ziyenera kuchitika tsiku ndi tsiku. Mnjira imeneyi tidzakhala kachisi wa Mulungu munjira imeneyi opembedza oona a Mulungu adzapelekedwa mu mitima yathu.

Tilankhure za kulambira mwa kamphindi chabe, lero sitifunanso kukhala ndi nsembe yanyama. Kodi ndi nsembe yotani yopelekedwa kwa Mulungu? Monga mwa baibulo, nsembe yopelekedwa ndi mtima yathu. Ife sindife nsembe ya kufa ndi nsembe ya mvyo. Maganizo athu sali ngati maganizo adziko lapansi, tiyenera kuganiza ndi maganizo a Kristu. Tiyenera kudzipereka tokha kwa Mulungu. Tidzakhala nsembe za moyo. Kumeneko ndiye kupembedza Mulungu, ngakhale sitikuimba kapena kupemphera. Tingapembedze Mulungu pamene tili kugwira nchitho. Tingapembedze Mulungu pamene tikuphika kapena kuchapa zobvala kapena kukhala pansu ndi anzathu.

Ngati tili ndi maganizo amene amalamulidwa ndi Yesu ndipo tizipeleka tokha monga nsembe tikupembedza Mulungu. Abale ndi alongo amenewa ndiye Ufumu wa Mulunguosati malo, osati nthawi, koma anthu. Anthu amene ali monga ansembe a Mulungu nthawi zonse tsiku lonse kulimbikitsana ndi kuthandizana wina ndi mnzake kuti akonde Mulungu ndi mtima wawo wonse maganizo, umunthu ndi mphamvu, choncho kuti apeleke miyoyo kwa Iye tsiku lili lonse. Ichi ndi cholowa chathu monga anthu ake. Tingakhale munjira imeneyi sitifunikanso kukhala monga chithunzi chija. Tingakhale munthu weni weni. Izi ndi zinthu zimene Mulungu afuna kwa ife lero. ndizimene mufunanso? Chabwino, tiyeni tiphunzire kukhala monga choncho pamodzi.

Kumanga Molingana Ndi Makonedwe

Ndikudziwa kuti zambiri zimene mwamva lero, zingakhale pang’ono zobvuta. Koma taona dziko lonse lapansi kuti ndi uthenga wabwino. Tabwera Unifu kwa tili osangalala kukuuzani njira imene Mulungu akhala akufuna kumanga nyumba yake. Takumana ndi anthu ambiri amene ali abwino. Enandi Achi pentekosti, ena ndi bapalisti, ndi ena ndi azipembedzo

zina. Akhala akusiyanasiyana miyoyo yawo yogawidwa kuchokera kwa wina. Akhala ndi miyoyo yawo yosweka ndi chimo. Choncho anthu ambiri ataya miyoyo yawo nd zokhumidwitsa ndi mgwirizano mu banja. Zokhumudwitsa zambiri zawoneka osati ngati Yesu. Ngakhalenso zokhumudwisa mwa ife tokha, zinthu zimene tikudziwa tiyenera kuchitira Yesu ngati sitichita. Chimo limene likufunika kuchotsa ndiye timapezeka tokha ofooka kuti lichoke.

Baibulo limati mu Yohane 3:8 kuti mwana wa munthu anabwera ku dziko kuononga chimo. Sanangobwera kudzakhulukira chimo lokha. Si choncho? Amen. Komanso akufuna tigonjetse chimo. Akufuna kutenga satana ndi kumugonjetsa pansu pa mapanzi ake. Ichi ndi cholowa cha ana a Mulungu, kuononga satana osati kungopulumuka, koma kuononga ntchito ya Mdyerekezi. Mwazina zimene sitinawone Mulungu akuonekera kuchilitsa mitima yosweka ndi kuwononga chimo, si chifukwa palibe anthu odabwitsa - alipo, sikuti palibe mphatso zabwino mu thupi la Khristo - zilipo mphatso zambiri. Zambiri zotere zachitika chifukwa zikhumbo za mitima zalephera kukondweretsa Mulungu chifukwa chosamanga mu njira ya Mulungu.

Chithunzi chimene takamba za nyumba za Mulungu. Kachisi ya Mulungu mu chipangano chakale chinayenera kumangidwa ndi maonekedwe. Mulungu anawauza m'mene angamangire kachisiyo, ndi kumanga munjira ya Mulungu imene adanena. Zinakhala zotani ngati anakatenga miyala yonse ndi Golide wa kachisi ndi kuchita m'mene amafunira? Mulungu sanakakondwa ndipo nyumba bwezni itagwa pansu.

Tikufuna kulankhula m'mene anthu angafikire kothekera kotere tsopano. Tingalote mphatso mu thupi la Kristo kumangidwa pamodzi kukhala mokhalirapo Mulungu, kudzazidwa ndi ulemmero wa Mulungu. Ilipo njira imene Mulungu akufuna kuti timange kuti mphamvu ya machimo siphwasulidwe mu moyo osati waukaporo ku zofooka zathu. Lingaliro la Mulungu ndi kumanga ife mu kulumikizana osati kukhala ndi mabvuto nthawi zonse. Mulungu ali ndi njira yodabwitsa pomanga nyumba yake ndi anthu ake odabwitsa chipembedzo mu dziko, mphaka tsopano, zakhala zomangidwa mu zolakwika, ndi anthu ena monga mabwana ndi anthu woyera ndi kuchita misonkhano ndi kumasulira kwawo kuti "Mpingo".

Mu dziko lowonekali, taphunzira kwa zaka ndithu m'mene tingamangire ndi zolimba. pali muyezo wa mchenga ndi kupita mu (Konterete) ndi madzinso pang'ono. Ngati mukathira simenti kapena mchenga wambiri konkrete silimba. taphunzira kuzungulira dziko lapansi kuti tipange konkrete wamphamvu muyenera kuika zitsulo zolimba mu izo kuti pasakhale ming'alu pamene pakhala kutentha ndi kuzizira. Tikudziwa kuti ngati tipanga njerwa kapena zidina, pali njira zina zimene timamangira nyumba ndi m'mene tingaikire njerwa mu ng'anjo. Pali zinthu zambiri taphunzira pazomanga mu dziko lino. Sitinadziwe m'mene tingamangire koma tsopano tiyenera kudziwa kumanga. Mulungu anati tiyenera kusamala m'mene tikumangira

Choncho, mwachiyembekezo mu chisomo cha Mulungu tidzalankhula zambiri pa kanthawi inai. M'mene anzathu amisiri Engineers anaphunzilira m'mene angagwiritsire ntchito konkerete mmene angakhalire wabwino kuti akhale wa mphamvu, momwemonso anthu a Mulungu ayenera kudziwa m'mene kumanga kwabwino kuti ikhale yolimba. Anthu abwino wokhala ndi mphatso zabwino amamanga bwino amamanga nyumba yotamandika ndi zimene timafuna kulankhulapo. m'mene tingamangire nyumba ya Mulungu bwino ndi anthu abwino omwewo. sikuti tikunyoza zakale, sitikudanana ndi machitidwe akaleyo, ndi mtima odzichepetsa tikungofuna kunena ndi nthawi yoi tipirire mstogolo tsopano. kale ndi kale tiyeni tikule msinkhu tsopano mu chikondi ndi kudekha mtima ndi kukoma mtima. Tiyeni tiyende pastogolo tsopano taonong zaka zambiri kukhala ana a chaka chimodzi. Ndi nthawi yoti tiyende tsopano, ndi manja athu otseguka.

Mzimu woyera watipatsa ise zoti tiganize ndingofuna kuwonjezera ndi mau achilimbikitso kanthawi kena tinayimba ndi nyimbo zina zinali za muchingezezi ndipo ndimadziwa m'modzi mwa nyimboyi inali "Ambuye ndinu olemkezeka, ndikudziwa kuti ndinu olemkezeka" ndi nyimbo yoona. Yesu ndi olemkezeka. Ndikuganiza malembo mu 1 Petro 2:9 koma ndinu mbadwa zasankhidwa, Ansembe a chifumu, mtundu woyera, anthu mwini wake Mulungu kuti mukalalikire zolemekezeka za iye amene akuitanani inu kuchoka mu mtima ndi kulowa mu kuwala kodabwitsa" Ambuye athu Yesu watiitana ife kuchokera mu mdima ndi kulowa mu kuwala, ndipo ndife othokoza. Muli othokoza inunso? Amen. Mukufuna

kuti mulengeze kuti ali olemkezeka? Alipo anthu ambiri otizungulira amene akufuna kumva kuti Ambuye Yesu ndi olemkezedwa. M'mawa uno tinadutsana ndi achisilamu, kodi mukufuna kuti adziwe kuti Yesu ndi olemkezeka? Ndikufuna kuti adziwe zazimenezi.

Kuzungulira dziko lapansi pano tapeza anthu amene amapembedza anthu akufa kapena mafano ndi enaso amene sapembedza chili chonse. Akufunika kuti adziwe kuti Yesu ndi olemkezeka, ndi ntchito yathu kukawawonetsa. Koma nkhani iyi yoonetsa Yesu kuti ndi olemkezeka ndi zotengera m'mene ife tili osati kulankhula chabe, m'mene Peturo anati pano. Anati ife ndi "Ansembe a talankhula zimenezi kum'mawaku kuti sikuti pali wansembe m'modzi yekha koma ansembe ambiri ndi kunenanso kuti ndife mtundu wapadera, anthu ake a Mulungu. Kunenanso kuti pakati pa Akristo Ambuye Yesu ndi mfumu ndipo timamumvera iye mu iey tidzalengeza matamando.

Ine ndimakhala ku Amerika, pa ulendo wathu ndabweretsa chitupa cha Amerika. Koma sindine, mukuona kwenikweni ndine mbadwa ya America. Ine ndine mbadwa ya ufumu wa Mulungu. Inu ndinu mbadwa za Malawi, koma a ufumu wa Mulungu, mwa choncho mbadwa za ufumu wa Mulungu ali mbadwa zabwino mu dziko lawo chifukwa amamvera malamulo osati kuchokera mu mantha koma kufuna kumvera basi. Koma ngati dziko lawo linena kuti asamvere Mulungu amati "Ai sitidza tidzamvera Mulungu osati munthu" Ndizimene zimathandauza kukhala mbadwa zosankhidwa. Munjira imeneyi sitidzalora chikhalidwe chathu kuti uza ife zochita. Tidzalora Mulungu kuti uza zochita. Ndikuchokera ku dziko lomwe chikhalidwe chake ndi cha uchimo chikhalidwe cha Amerika chaiwala kuchita manyazi ndi chimo. Sindidzamvera chikhalidwe changa. Ndidzamvera Mulungu Amen.

Ine sindidziwa chikhalidwe chachi Malawi komanso inunso muyenera Mulungu, osati chikhalidwe chanu. M'menemondiyembaliyokhalamu ufumu wa Mulungu. Chomwechonso ndi zoono ndi chipembedzo. Lero m'mawa tadutsa nyumba yolembedwa "Mpingo wa Nazarene" Ndikudutsanso malo ena otchedwa Luzarene" Tinadutsanso pena analemba "Mpingo wa Khristu" onsewa akukumana lero. Onsenso ali kustatira miyambo yawo. Mbali ina ya Ufumu wa Mulungu ndi kumvera Mulungu koposa miyambo chabe Amen? Miyambo sali mfumu yathu, Yesu Khristu ndiye mfumu yathu. Tili mtundo wapaderadera, tidzaimba ndi kulengeza olemkezeka Yesu Kristo. Ndife

mtundu woyera. Zolengeza zahu ndi zomverka bwino, sizosokoneza, ndipo amuna onse adzafunsidwa ngati adzapinde mabondo awo ndi kumvera iye. M'mawa uno sitinabweretse chipembedzo china chatsopano. Tabweretsa ufumu wa Mulungu, tiyeni tikhale munjira imeneyi tonse, AMEN.

Madziko Anayi A Choonadi

Salima, Malawi, Africa, October 3, 1999

(Izi zidayankhulidwa ndi abale atatu pamene adayima pamudzi wina ku Malawi ku africa, pakuonetsera zokhudza mpingo ya chipentekositi. MUTSIKU LIMODZI “Mpingo” wonse udatembenukira kwa Yesu ndipo siwunayang’anepo m’mbuyo. Polipilira mtengo waukulu, munthu ali yense payekha, zosintha zambiri zidapangidwa kwamuyaya, kusintha anthu ambiri, ndikhalenso gawo lawo laza chuma m’mudzi wawo kumagulu ena achipembedzokuti china chake chodabwitsa chikuchitika pakati pawo. Ndikufunitsitsa kukadakhala kotheka tikadajambula zinthu zomwe zidanenedwa ndi abale ochokera m’mudzi umenewu ku Africa muolu lotsatira patatha nthawi imene maganizo awa adayikidwa ndi oyera mtima kumeneko. Ichi chidali ndipo ndichodabwitsa ndi, ndithudi, kuwona kulimbika mtima kwao ndi “changu chao pa nyumba ya Atate” zowonetseredwa ndi “chikondi cha choonadi” ndi machitachita munthawi kuchokera pa tsiku limenelo.)

Chuma chamtengo wapatali ndi kudzutsa ndi kuchangamutsa anthu a Mulungu padziko lapansi munthawi yino. Chilimo chilungamo chapadera chomwe chakhala chili m’Baibulo lanu nthawi yonseyi chimene chidzasintha moyo wanu ndikusinthanso njira imene mpingo umaonetseredwa, kuti koposaposa tikakweze Mfumu Yesu ndikuwona loto lake likukwaniritsidwa. Ndichiyembekezo chathu, mwa mzimu oyera, kuti maso athu onse akatseguke ndikuwona choonadi chokongola ichi. Mulungu akufuna kumanga nyumba yake kuti tonse tikhale amphamvu pamodzi. Iye akufuna kumanga nyumba yake kuti makomo a ndende asadzailakenso konse. Iye akufuna kumanga nyumba yake kuti ubale ukhonze kuchilitsidwa. Iy akufuna kumanga nyumba yake kuti iye akhale omasuka kuchiza matupi athu, malingaliro athu ndinso moyo yathu. Iye akufuna kumanga nyumba yake kuti ife tikhale amphamu ndi nzeru, ndi kuti uthenga wabwino wa Yesu upite patsogolo, mwamphamvu kuposa kale.

Kodi muli nako kulimbika mtima pakumva zinthu izi? Kodi mumvera mau a Mulungu pamene mukumva zinthu izi? Kodi mwasintha miyoyo yanu posawerengera mtengo wake? Ngati muli nako kulimbika mtima kuti mumvera ndi kudzipereka, ndiye chonde werenganibe.

Pali choonadi chinayi chimene ife tiyenera kumangapo. Popanda chimenechi, nyumba ya Mulungu sidzakhala yamphamvu, ndipo makomo a ndende adzapitiliza kudzetsa chisokonezo pa nyumbayi. Komabe, ngati ife timvetsetsa zinthu zinayi izi ndikuzimvera izo, ndipo ngati ife tifunitsitsa kudzipereka, ngakhale chowawa chidze, pa choonadi cha Mulungu chinayi chimenechi, kenako Mulungu adzalemekedwa ichi ndipo iye adzatumidza mphamvu yake mumiyoyo yake. Osauka adzachita bwino ndipo ofooka adzapeza mphamvu. Uwu wakhala uli mtima wa Mulungu ndi cholinga chake. Komabe, chuma ichi chokhala chitabedwa kuchokera kwa ife kuchokera mzaka zoyamba mpaka tsono. Ife talandidwa ndi miyambo ya anthu yachabechabe.

Choonadi Choyamba: Kodi Mkhristu Ndi Ndani?

Choonadi chamadziko choyamba ndi kufotokoza moyenera chimene mkhristu ali. Ife takhala tili otayirira padziko lonse lapansi ndi mumiyambo yonse pazokhudza ichi. Chifukwa takhala osadziwa mwachindunji zokhudzana ndi chimene Mkhristu ali, tamanga kwambiri kwa nyumba ya Mulungu pa mchenga. Ifeyo tafotokozera ndi kutanthauzira zimene zimampangitsa munthu kukhala Mkhristu kudzera mu zinthu zomwe sizenizeni, kapena mamvedwe a matupi athu kapena mmene timalerera banja. tatanthauzira chimene Mkhristu kudzera mkati ngati wina amayimba bwino, kapena amakhala nawo m'misonkhano kwambiri, kapena amapereka chakhumi bwino. Umo sim'mene Yesu adatanthauzira Mkhristu.

Yesu adati, “Pokhapokha inu mutataya zonse, simungakhale ophunzira anga.” Yesu adati “pokhapokha inu mutasenza mtanda wanu tsiku ndi tsiku, simunganditsate ine.” Mubukhu la Machitidwe, Baibulo limati, “Ophunzira adatchedwa ‘akhristu’ koyamba ku Antiyokea. Tsono pamene muona liu loti ‘ophunzira’ muziphunzitsa za Yesu, ganizirani mumalingaliro anu zaliu loti, “Mkhristu” pamene Yesu ananena kuti,

“pokhapokha mutataya zonse, simungakhale ophunzira anga” *Iye amatanthauza kuti simungakhale a Khristu ngati inu simutaya kapena kupereka moyo wau.* Iye sadanene kuti, “pokhapokha mutakhala nawo mumisonkhano, simungakhale a Khristu” Iye adanena kuti, “pokhapokha mutafa kwa inu nokha, simungakhale a Khristu.

Yesu akuyitana kwa anthu amene adafa kwa iwo okha. Iwo adzataya chili chonse nkumutsatira iye. Iwo adzataya kunyada kwawo ndi chuma chawo kuti amutsatire iye. Iwo adzatembenuka kumachimo awo ndi kudzikonda. Iwe adzakonda ena koposa m'mene amadzikondera eni. Ubale umenewu wapakati pa iwo ndi Yesu udzasintha m'mene amachitira zinthu zawo tsiku liri lonse.

Pokhapokha ife titanthauzira liu loti “Mkhristu” munjira yomwe Yesu atanthauzira, nyumbayi idzatitimira mumchenga ndikukokoledwa. Leli ndi chimene Yesu Mfumu adalonjedza kuti chidzachitika tikamanga pa mchenga wa kumva, kuyimba ndi kuyankhula, koma osamvera. Nyumba imene timanga idzakhala, mwina chinthu chimene chili chongosangalatsa ife, koma sochidzatanthauza kanthu kwa Yesu. Nyumba imene timanga ikonza kutisangalatsa ife chifukwa tikuyimba ndi kukhala pamodzi, koma siyitanthauza kali konse ngati Mulungu siali okondwa nayo. Sichitanthauza kali konse ngati satana akadagonjetsabe pa nkondoyi m'miyoyo yathu. Ngati ife sitimanga moyo ndi Mpingo zomwe zibweretsa kusangalala kwa Yesu, ndiye kuti ife tikungotaya nthawi yathu ndi nthawi ya Mulungu.

Mkwingwirima yake

Mwala wa madziko oyamba pakumanga nyumba ya Mulungu ndi kufotokoza chimene Mkhristu ali munjira yomwe Baibulo limafotokozera chimene Mkhristu ali. *Ife tiyenera kupanga chisankho mwakulingana ndi amene Mulungu amamutcha Khristu.* Kodi munthu nkutheka kukhala membala wa Mpingo wa Mulungu koma osakhala Mkhristu? Nzosatheka! Koma pa dziko lapansi anthu akuphunzitsidwa kuti ndi zabwino bwino kuti Mkhristu ndi amene siali Mkhristu kukhala gawo la Mpingo. Baibulo limati ichi sichoona! Mu Akorinto oyamba 5, Baibulo limati “chotsani dzotupitsa mumkate” chotsani tchimo mu Mpingo. Ichi ndi chofunikira kumvetsetsa, chifukwa Mulungu adati, “chotupitsa pang'ono chimatupitsa mkate onse”

Kodi inu mukukumbuka pamene malinga a Yeriko anagwa pansi? Anthu a Mulungu adali a mphamvu munjira yodabwitsa. Komabe, patangotha kugwa kwa malinga a Yeriko, Israel idagonjetsedwa pankhondo. Iwo adamenyedwa! Nchifukwa chiyani, Israel idagonjetsedwa pa nkhoodoyo? Chifukwa choti munthu mwa Israel adachimwa mu hema yake. Mulungu adakwiya chifukwamunthu m'modzi mu Mpingo wonse adachimwa mumoyo wake umene udabisika. Munthu ameneyu, Akani, adali ndi fanizo (mulungu osema) litakwiliridwa pansi pa hema yake. Mulungu adapangitsa a *Israel onse* kuvutika ndi chigonjetsedwa chifukwa cha tchimolo. Mulungu ali yemweyo dzulo, lero ndi kunthawi zonse. Sichoncho? Mulungu akadali osakondwa pamene anthu mu Mpingo wake abisa tchimo miyoyo yawo. Ichi chimaswa mtima wake. Baibulo linena kuti Mulungu amabweretsa chiweruzo pa ichi.

Kodi ndi chabwinobwino kwaife kunena kuti wina wake amene sadapereke moyo wake kwatunthu kwenikweni kwa Yesu akhonza kubwera ndikukhala mbali ya Mpingo? Ayi! Ichi ndi chibwana kwambiri. Mulungu amabweretsa chiweruzo pa nyumba yonse chifukwa cha munthu m'modzi amene akunamizira kukhala Mkristu, koma sanapereke moyo kwatunthu kwenikweni kwa Yesu. Tsono, ngati ife tikufuna kuona Nyumba ya Ulemerero imene imagwira ntchito ya Mulungu, chinthu choyamba chimene tingachite ndikutanthauzira liu loti “Mkristu” munjira yomweyo yomwe Yesu anenera. malemba anena “pokhapokha mutataya zonse, simungakhale ophunzira anga” “Ngati mukonda abambo, amai ndi ana anu koposa ine, simungakhale ophunzira anga, ngati mukonda dziko lapansi ndi zinthu zamdzikoli, mwasanduka mdani wanga, Mulungu amadana ndi odzitamandira ndipo amapereka chisomo kwa odzichepetsa”.

Ife tiyenera molondola, kutanthauzira chimene Mkristu membala wa Mpingo - ali chenicheni! Inuyo simunganamizire kusambitsidwa mu mwazi wa Yesu, ndi kukhala chiwalo cha thupi la Yesu ndi kuyesedzera kuti Mkristu ngati mtima wanu siuli kwa Yesu pamene muli kunyumba, kapena kuntchito, kapena m'minda. Ngati ubale wanu siuli ubale oyera, muyenera kulapa ndi kupereka moyo wanu kwa Yesu.

Choonadi Chachiwiri: Kodi Utsogoleri Nchiyani?

Chinthu chachiwiri chimene tiyenera kutanthauzira, mwala wachiwiri wa madziko pakumanga Nyumba ya Mulungu, zikhudzana ndi chimene utsogoleri mu Nyumba ya Mulungu. Ichi ndicho choonadi chodabwitsa kwambiri! ichi chidzabweretsa chimwemwe pa inu ndi kusintha moyo wanu. Mu maiko padziko lonse lapansi, tapanga chibwana chachikulu kwambiri pankhani yokhudza utsogoleri mu Mpingo. Mumalo ambiri munthu amene adaphunzira Baibulo ku seminale kapena kusukulu ya Baibulo, kapena odziwa zamalonda kapena odziwa kuyankhula amapatsidwa “ubusa”. Ife taona ku India ndi maiko ena kuti nthawi zambiri, munthu amene ndi njinga amenenso angathe kuwerenga amasankhidwa kukhala mtsogoleri. Ichi sinjira ya Mulungu! utsogoleri wa Mulungu siugona pa iwo amene angathe kuyankhula bwino, kapena amene ali ndi luso pa malonda, kapena amene ali ndi chuma kapena maphunziro kapena mankhwala kapena maonekedwe abwino kapena njinga.

Kukhala monga Yesu

Ine ndikupatsani chitsanzo kuchokera mumalemba. Machitidwe 6, padali azimayi amasiye achi Greek amene amakhala anjala kwambiri kwa nthawi zambiri chifukwa choti amayiwalidwa. Pamene chakudya chimagawidwa iwo amasiyidwa ndi kusalidwa bwino. Mpingo mu Yerusalemu adayenera kupanga ganizo la m'mene akadathetsera vuto ili. iwo adaganiza kuti asankhe anthu ena kuti athetse vutoli. Ngati mungawerenge Baibulo lanu, mupeza kuti padali njira ina yosankhila anthu amenewo. Kodi Baibulo likunena kuti, “sankhani kuchokera pakati pa anthu asanu ndi awiriwa amene amadziwa ma Baibulo awo? Ayi. “Sankhani kuchokera pakati pa anthu asanu ndi awiri amene angayimbe bwino?” Ayi, sankhani kuchokera pakati pa anthuwa amene ali ndi luso pa malonda, kapena pa malonda a zakudya? Ayi, “Sankhani kuchokera pakati pa anthuwa amene akhonza kuyankhula bwino?” Ayi. Njira yothetsera vutoli idali, “zisakhalire kuchokera pakati panu anthu asanu ndi awiri amene ali ozadzidwa ndi Mzimu oyera ndi ozadzidwa ndi nzeru.

Awa adali anthu amene amayesedwa tsiku liri lonse. Awasadali anthu amene adapita kusukulu kuti akhale auzimu, kapena amene amangoyankhula bwino chabe. Awa adali anthu amene adali abwenzi a Mulungu ndiposno

abwenzi akuya abale ndi alongo apakti pawo tsiku liri lonse. Stefano ndi Filipi ndi anthu asanu ndi awiri awa amapezeka mnyumba za anthu tsiku liri lonse, kuyetsetsa kuthandiza anthuwo. iwo amakhonza kugwira manja a ana a anzawo ndikuyankhula nawo ndi kuwaphunzitsa. iwo amakhonza kutungira madzi okhulupirira ena ndi kuwathandiza iwo. Iwo amakhonza kupita kunyumba za anthu pamene iwo akutaya mtima. Iwo amakhonza kupita m'malo ogwira ntchito a anthu mkati mwa tsiku ndikukawalimbikitsa iwo. Ndi iwo sadali ngakhale kutchedwa atsogoleri! iwo adali abale chabe amene amakhala umoyo wa Yesu tsiku liri lonse. “Zisankhileni nokha kuchokera pakati panu anthu asanu ndi awiri amene awoneka ngati Yesu, asanu ndi awiri amene angathe kuona Mulungu ndi kumva Mulungu.” Sankhani anthu asanu ndi awiri amene akutsuka mapazi a oyera mtima tsiku liri lonse”. “Abale asanu ndi awiri amene ali abale chabe tsiku lirilons amene amakodna Mulungu mozama kuchokera pansu pa mtima ndi kuonetsera kulumikizika kodabwitsa kwa Messiah.”

Chifukwa anthu amenewa awoneka ngati Yesu, tsiku liri lonse munyumba za anthu, ndiye kuti ife timadziwa kuti iwo ali odzadzidwa ndi mzimu oyera. Iwo siali odzadzidwa ndi mzimu oyera chifukwa choti iwo amayankhula mokweza kapena kuyimba bwino kapena amayankhula zinthu zambiri. Iwo ali ozdadzidwa ndi mzimu oyera chifukwa choti iwo amayankhula mokweza kapena kuyimba bwino kapena amayankhula zinthu zambiri. Iwo ali ozadzidwa ndi mzimu oyera wa Yesu **chifukwa choti iwo amaoneka ngati Yesu ndi moyo wawo wa tsiku ndi tsiku**. Uwu ndi mtundu okhawa wa utsogoleri m'Baibulo. Mu chipangano cha tsopano, Yesu adauza atumwi khumi ndi awiri aja kuti asatchule munthu kuti mphunzitsi, tate, mtsogoleri, mbuye, rabbi, m'busa, pakuti onse ndi abale! Tsopano ife tili ndi maganizo odabwitsa, osiyana a utsogoleri.

Zosiyana ndi zadziko lapansi

Kuphunzira ichi chidali chovuta kwambiri kwa ine pandekha. Muzaka zambiri zapitazo ndidali “m'busa” kufikira nditazindikira zimene Baibulo lidanena, zoti ndimayenera kungokhala m'bale pakati pa abale. Ndimayenera kugwiritsa ntchito mphatso ili yonse ndingakhale nayo “pakati pa abale, monga m'modzi amene atumikira” - osati monga bwana kapena wina wake oti adzioneredwa panthawi zonse. Ngati chimenechi

chidali choona kwa Petro, Yohane, Yakobo ndi atumwi ena, chiyenera kukhalanso choona kwa wina ali yense wa ife, opanda kuchotserapo! “Muli nonse abale chabe.”

Ndidatuluka kuchokera ku ndalama zambiri zomwe ndimapanga mudziko lamalonda pakukhala “m'busa”. Ndipo tsopano ndidayenera kusiyana nazo ndalama ndi mipando yakukhala osati monga mwa Baibulo imene anthu amaitcha “M'busa” wa mpingo. Ndidayenera kupanga chisankho kuti ndiyenera kukhala *m'bale pakati pa abale*. Chili chonse chimene Yesu wapanga m'moyo wanga chikaonekera munyumba ndi m'miyoyo ina pamene ndigwirana manja ndi ana. Ine sindimayeneranso kukhala chipolopolo chachikulu ayi. Sindimayenerera kukhala munthu wamkulu ayi. Ndikadangopanga zimene Paulo adanena kuti adapanga ndi Atesalonika, ndi Afilipi, ndi okhulupirira mu mzinda wa Korinto ndipo chimenechi ndiko kukonda anthu monga tate ndi m'bwenzi, ndiponso monga m'bale kuchokera nyumba ina kufikira nyumba ina.

Paulo adati, “Ndidapita kuchokera nyumba kufikira ina ndi misonzi” *Iye adakonda* anthu monga tate, kapena monga m'bale. Iye analera m'moyo yawo monga mai angalerere mwana okhulupirira ena adamichitiranso iye chimodzimidzi, uwi ndiye utsogoleri wona mu Mpingo Owona wa Chipangano Chatsopano.

Yesu adati kwa atumwi, “Amitundu ali ndi njira ina yokhalira ndi utsogoleri, koma izi siziri choncho ndi inu.” Mu mpingo woonadi, Mpingo umene makomo a ndende sangaulake, *utsogoleri wake ndi wosiyana kwambiri ndi njira ya dziko lapansi*. Utsogoleri umabwera kuchokera mkati kati, osati “kuwupatsa mphamvu” kuchokera pamwamba.

Mphatso ndi ulamuliro wa Yesu

Ndiloleni ndikupangireni chithunzi inu. Baibulo limanena ku Aefeso 4 kuti pamene Yesu adakwera kumwamba, iye adapereka mphatso kwa anthu. Yesu adatenga mphatso zonse zimene anali nazo (ndipo Yesu anali ndi mphatso zauzimu zambiri, sochoncho kodi?) ndipo iye adapereka mphatsozi kwa anthu ake onse. Iye sadatenga mphatso zonse zimene adali nazo ndikuziyika pa “m'busa” kapena pa “munthu m'modzi wa Mulungu” Malembo akunena kuti iye adatenga zonse mwa mphatso zake ndipo

adazipereka izo kwa thupi lake lonse. Baibulo linena kuti mzimu uyikidwa ndi kuperekedwa ngati mphatso, monga mwa amene Mzimu ufunira, pa Mpingo wake onse. Ngati inu muli Mkristu oona, ngati mwatayadi moyo wanu chifukwa cha Yesu, ndiye kuti Mzimu oyera ukupatsani inu mphatso yapadera uoposa. Mphatso yanu ndi gawo kapena kuti chiwalo cha Yesu.

Yesu asadapite kubwerera kumwamba, adati, “ulamuliro onse ku Mwamba ndi padziko zapatsidwa kwa ine” Kodi mukukumbuka kuti Yesu adanena zimenezi? Ulamuliro onse uli kwa Yesu ndipo osati wina ali yense! Tsono ngati Yesu anapereka gawo la iye yekha kwa inu, gawo lina kwa munthu uyu ndi gawo lina kwa munthu uyo, ndiye kuti mphatso yauzimu ina ili yonse adapereka kwa wina ali yense wa inu, pali ulamuliro mu mphatso imeneyo. Yesu adapereka mphatso ndipo iye ali ndi ulamuliro onse.

Pali mphatso zamitundu yambiri zomwe zidalembedwa m’Baibulo. Mzimu Oyera, mwachitsanzo, umapereka chifundo ngati mphatso. Mphatso ya chifundo ndi gawo la Yesu limene iye adapereka kwa anthu ena. Ndi mphatso yodabwitsa. Tonse a ife tiyenera kukhala ndi chifundo, sichoncho? Koma pali chifundo chodabwitsa chimene chili mphatso ya Mzimu Oyera. Tsono, ngati iye adapereka kwa inu mphatso yapadera ya chifundoyi, inu mwapatsidwa ulamuliro kumbali ya chifundo. Ngati inu muli ndi mphatso yodabwitsa ya chifundoyi ndipo ine ndilibe, ndipo ngati ulamuliro onse uli kwa Yesu ndi inu muli ndi mbali ya Yesu, ndiye kuti ine ndilemekeze mphatso imeneyi mwa inu. Muli ndi ulamuliro kumbali imeneyo. Kodi mukumvetsetsa? Ichi ndi chimene utsogoleri uli!

Ulamuliro onse uli kwa Yesu ndipo ife tonse tili nayo mphatso zathu zapadera. Mwachitsanzo, pali mphatso ya uphunzitsi. Ahebri 5 imati, “tonse tayenera kukhala aphunzitsi tsopano” Komanso ku Aefeso 4 ndi Aroma 12 limati pali mphatso zauzimu za uphunzitsi zimene Yesu amapereka. *Ichi chitanthauza kuti pali ulamuliro mu mphatso imeneyi chifukwa Yesu amapereka mphatsoyi ndipo Iye ali ndi ulamuliro onse.* Ife tidzipereke kwa wina ndi mnzake mu ichi. Koma kuphunzitsa ndi gawo limodzi lokha ndi mphatso imodzi yokha ya Yesu. *Palinso mphatso zina zambiri.* Pakuti ulamuliro onse uli kwa ali yense wa ife ndi gawo la Yesu, ndiye tikuyenera kudzipereka ku mphatso zomwe zili mwa wina ali yense wa ife chifukwa Yesu ndi amene waikamo mwa ife mphatsozi.

Palibe ulamuliro wina wake umene uli mwa “munthu wa Mulungu” m’modzi ndipo wina ali yense angokhala chabe ndikuonerera. Chifukwa chanjira zimene anthu amangira Mpingo zaka zodutsa 1800 zapitazo, ife takhala ndi machitidwe onga ngati pali mphatso imodzi yokha basi - mphatso ya “ubusa”. (Kapena mwina wina ali yense ali oloedwa kukhala ndi mphatso yopereka ndalama yokha!) Koma m’busa / ubusa ndiye mphatso yokha basi! Ngati ife timanga molakwika, tonse tiluza. Ngati, munthu m’modzi akankhilidwa kutsogolo kukhala “m’busa” ndipo wina ali yense kungokhala pansu ndi kumvetsera nthawi zonse, ndiye kuti wina ali yense sakugawana nawo mphatso yanuyo. Iwo amangotenga mphatso “ya ubusayo”. Ichi ndi chochepa kwambiri ndi chachinyengo! Ngati tikufuna kuti tione ukulu wa Mulungu, ndipo ngati tikufuna kuona miyoyo yathu yonse ikusintha ndipo miyoyo ya ana athu ikusintha, apa ife pafunika zigawo za Yesu, Amen? Ife sitiyenera kukhazikika pa gawo chabe la Yesu. Amen?

Kulimbika mtima kukusintha ndi kulimbika mtima kukuthamanga

Kodi mukuona chifukwa chimene tikunenera kuti tiyenera kulimbikira mtima? Zinthu ziyenera kusintha! Simungapitirire kuchita zomwe mwakhala mukuchita. Mupanga chisankho kugwiritsa ntchito mphatso yanu kwambiri ndiponso kulandira enanso kuti nawonso atero. Mupanga chisankho kukhala omvera ndipo kukhala ndi kulimbika mtima. Ngati mupitirira kukhala pa mpando wanu kapena pansu nthawi zonse ndiponso osagwiritsa ntchito yanu kwambiri ngati mmene zimayenera kukhalira, mphatso yanu idzapitirira kulowa pansu. “Iye amene wapatsidwa mphatso akuyenera kuonetsa kukhulupirika.” Kodi mukukumbuka zimene zidachitika kwa munthu amene adakwirira talente yake? Yesu adati, “Iwe oipa, wantchito waulesi.” Icho ndi chimene Yesu amanena kwa ife pamene ife sitipanga zomwe tiyenera kuchita. Ngati ine sindigwiritsa ntchito mphatso yanga kapena inu kugwiritsa ntchito mphatso yanu, ife tili “oipa ndi aulesi”.

Kodi mukuona m’mene miyambo ya anthu ikubela ndi kulanda mau a Mulungu? Bwanji inu mutakhala othamanga wa Olympic mwagona pa bedi ndi wina wake watenga chingwe ndipo wamanga kuzungulira inu pamodzi ndi bedi? Ngakhale mutakhala opambana pamasewero olimbitsa

thupi, ngati inu mwamangidwa pamenepo pamodzi ndi bedi minofu yanu ikulungala ndipo kenako inu mufa. Mphamvu ndi kuthekera kwanu konse kupita pachabe chifukwa mwamangidwa kubedi kwa miyezi kapena zaka. Kodi inu mukuona m'mene miyambo ya anthu imabela ndi kulanda Mau a Mulungu? Njira imene tamangira mzaka zoposa 1800 mu Nyumba ya Mulungu zamanga anthu a Mulungu ambiri kumodzi ndi bedi. Iwo akhala opanda kuthekera koima ndi kothamanga ndi kokwaniritsa masomphenya awo chifukwa anthu amanga molakwika, mosatsatira mau a Mulungu. Ngati ife tamanga kapena kukonza Mpingo munjira imene makweza munthu m'modzi kapena "waudindo" ndi kuzima mphatso zaena, ife tili zigawenga mu Bwalo la milandu la kumwamba chifukwa cha zowongeka ndi zowawa zimene ena awawidwa nazo chifukwa cha "chotupitsa mu mkate" ndiponso mphatso zosagwiritsidwa! Sikuti ndi chifukwa choti anthu ndi "oipa" chimene ife tamangira molakwika. Kwenikweni ndi chifukwa choti ife sitikudziwa kumanga Nyumba ya Mulungu ndi Mapangidwe ake.

Tsono kumbukirani kuti mwala omangira oyamba wa madziko oonadi ndi akuti okhawa ali *Akhristu oonadi* okhonza kuzitcha okha mamembala a Mpingo. Mwala wa madziko wachiwiri umene ungamange Nyumba ya Mulungu ndi kuti tiyenera kumvetsetsa utsogoleri bwino. Ife tayika munthu m'modzi kukhala olamulira kwa zaka 1800. Ife tatenga mphatso imodzi, mphatso ya "mbusa" (kapena ubusa, kutanthauzira kwabwino) ndipo tayipanga kukhala mphatso yoyambirira. Ichi ndi kutali ndi choonadi mu Mpingo mu Baibulo!

Ndipo sichiyenera kukhala chilungamo ngakhale pano. Ichi chamangirira ambiri mwa anthu a Mulungu ku bedi kuti iwo asakhalenso m'mene Mulungu adawaitanira iwo kuti akhale. Utsogoleri uli mwa anthu onse a Mulungu. Baibulo limatcha ife Ufumu wa ansembe. Baibulo silinanene kuti Ufumu okhala ndi ansembe, koma Ufumu wa ansembe. Palibe gulu lapadera monga ngati ansembe achilevi aku Chipangano chakale. Muchipangano chatsopano onse a anthu a Mulungu ali oyenera kukhala ansembe jwawina ndi mnzake. MULUNGU adati, "pemene bvumbulutso lidza kwachiwiri, siyani oyambayo akhale pansiiiiii!"

Ngati inu muli odzadzidwa ndi mzimu oyera ndi odzadzidwa ndi nzeru, ndiye kuti ndinu mtsogoleri.

Sikuti ndingoti unapita kusukulu, kapena ngati umayankhula bwino. Sikuti ndingoti uli wam'muna kapena wamkazi, kapena wamng'ono kapena wamkulu. Utsogoleri ndi munthu amene ali ndi mphatso ya Yesu ndi ubale ndi Yesu, adzadzidwa ndi Mzimu Oyera ndi nzeru. Utsogoleri ndi kugwirana manja ndi ana tsiku liri lonse. Utsogoleri ndi kuchiza mabala a anthu a Mulungu kuchokera nyumba ina kufukira nyumba ina tsiku liri losne. Utsogoleri ndi kuthandiza kuthetsa mavuto a tchimo mu miyoyo ya abale ndi kusambitsa mapazi awo tsiku liri lonse. Ichi ndi chimene utsogoleri uli ndipo ndi mtundu okha wa utsogoleri umene baibulo limankhula, kugwiritsa ntchito gawo la Yesu limene Mzimu Oyera udayikamo mwa wina ndi mnzake wa ife. Ichi ndi mbali ya utsogoleri ndi ulamuliro. Ichi chitanthauza kuti ife tiyenera kusintha m'mene timachitira tsopano. Ife tiyenera kusintha m'mene timaonera utsogoleri ndi m'mene ife timachitira pa ndondomeko ya utsogoleri.

Ichi ndi chosintha kwambiri. Ichi chisintha m'mene timachitira mu misonkhano yathu, m'mene ife timachitira mu moyo wathu wa tsiku liri lonse. pali mtengo omwe tiyenera kulipira pa ichi. Koma Mulungu amapereka mphoto kwa ife kokwana zana limodzi pa chili chonse timapereka, monga mwa lonjezano la Yesu.

Pamene ine ndidali "m'busa" ndidaganiza kuti ndikhale mosiyana ndi poyamba. Ine ndidaganiza kuti ndikhulupirire ndi kumvera malembo pazokhudza utsogoleri. Ndidasankha kukhala m'bale pakati pa abale koposa kukhala kutsogolo kwa abale. Kunena moona, ndidaopa. Ndidaopa za m'mene ndidzasamlira banja langa. Ndidaopanso kuti mwina ndidzataya ubale wanga ndi Mulungu mwinamwake ndi kuti anthu sadzandilemekeza inenso ayi. Ndidali ndi mantha pa zinthu zambiri. Koma ndidadziwa kuti Mulungu adanena mu Baibulo. Iye amafuna ine kuti ndikhale m'bale pakati pa abale. Mu moyo wanga wa tsiku ndi tsiku, sindidzakhalanso bwana ayi. Ndidzangokhala chabe m'modzi mwa abale, ndipo ndidzapitilira kugwiritsa ntchito mphatso yanga kuchokera kwa Yesu monga "m'bale pakati pa abale" amene mofanana agwiritsa ntchito mphatso zao. Izi zidasintha *chili chonse* pa ine, koma Mulungu adali okhulupirika kwambiri. Iye adalonjeza kuti palibe amene adasuya chili chonse amene adzalephera kulandira koposa zana limodzi kapena kuposa zomwe adataya. Mulungu amasunga lonjezano lake! Amen?

Kuchokera pa zintchito, ndikufuna ndiyikepo maganizo anga pa inu akuti ngati tifunitsadi kuti tilemekze mphatso zimene ziri mwa wina ali yense mwa ife, ndikutulutsa poyera mphatso zimene zili mwa anthu onse a Mulungu, ndiye tifunika kusintha zinthu zambiri. Monga mopusa m'mene chikumvekeramu, chimodzi mwa zinthu zimenezo chikhonza kukhala mmene timakhalira pamene tisonkhana pamodzi. Pamene Yesu anali pano, Iye adali ndi anthu omuzungulira Iye - awa ndiwo amayi anga, abale anga, ndi alongo anga” (Mariko 3) Kukhala mwabwalo omuzungulira Iye! Ichi sichinthu chachizolowezi kupanga, pamen ife tasonkha pamodzi kuti tumumve IYE, ndipo osati munthu chabe wa mphatso zowerengeka. Ichi chikhonza kumveka ngati chopepuka kwambiri kwa inu, ndi chikhonza kusamveka ngati cha phindu ndi chofunikira, koma ndikufuna ndikutsimikizireni inu kuti ichi ndi chofunikira. Ndamva kuti mau ayimira “Gome” ndi “mnofu” amanenedwa munjira imodzimodzi. chi Faransa.

Ngati wina wake kumalo ogwirira ntchito kapena kumsika anena chinthu china kwa inu, kodi chili ndi kanthu mmene achinenera? Zooni chili ndi kanthu! Ngati iwe akutsamira, kapena kukhala motsamira kumwala ndi kunena china chake motsitsa kwanaku akuyatsamula, chimenechi chikhala chosiyana koposa ngati iwo akadanena chinthu chomwecho ndi nkhope yao yoima moyang'anizana ndi yanu ndipo akuyang'ana m'maso anu ndi moto. M'MENE chili chonse chinenedwa chili ndi kanthu kwakukulu.

Pamene tikhala ndi wina ali yense akuyang'ana kutsogolo, chimabweranso kumvetsera konse kwa munthu m'modzi. Ife sitilinsu ofananana pakati pa ofanananso ayi. Ine ndili odzipereka kwa ali yense amene watenga mpando olamulira kustogolo kwa ine monga mbuye wanga, kapena kondakitara kapena wapolisi wamagalimoto kapena kadaulo wa china chake. Koma dziwani ichi bwino lomwe! Wantchito oona wa Mulungu sakhumbira kufuna kumveredwa pa iye yekha. Yohane mbatizi, amene adali munthu wa mphamvu obadwa mwa mzimayi adati, “Yesu ayenera akulire, ine ndiyenera ndichepere. Ine sindifuna anthu adziyang'ana pa ine nthawi zonse monga munthu amene ali ndi mayankho onse. Ine ndikungofuna kukonda ndi kutumikira Yesu, ndi kuthandiza ali yense kupanga ichinso. Yesu ayenera kukwezeka, ine ndiyenera kuchepera.

Munthu wa Mulungu awona ali yense amafuna kudziwenzeka kuti Yesu adzitengere ulamuliro koposa iye mwini. Ndiponso, ena adzanena kuti ichi

ndi chopanda tanthauzo, koma mukukhala mkuyenda kwanga m'mayiko ambiri ndi m'mizinda ndikutsimikizani inu, sikuti ndichosafunika. Ichi ndi chofunika kwambiri, m'mene tinganenera chinthu china chake. Pamene ife tiyika mipando m'mizere malo mwa mabwalo, ichi chikhonza ngati kuyatsa nyali pamunthu m'modzi. Ali yense amangokhala ngati odzangoonerera ndipo munthu m'modzi ndiye ali wachikoka. Icho ndi chinthu cholakwika chifukwa pali mphatso zambiri pakati pathu, ndipo pali zigawo zonse za Yesu. Ngati ife tiyika aliyense mwakuyang'ana kustogolo ndiye kuti likukwezga mphatso imodzi yokha basi. Kodi ndikunyada kwanji komwe munthu angakhale nako pakuzivomereza yekha nthawi zonse kukhala “mpando wa ufumu” kapena nyali younikira.

Tsono, bwanji ngati m'malo mwake mphatso zonse zitakhala ndi malo ofanana? Mwina pali wina wake ndi mphatso ya ubusa atakhala mwa bwalo. Mwina wina wake ndi mphatso ya uphunzitsi atakhala pamenepa ndipo wa mphatso ya chifundo atakhala pamenepa. Mphatso ya kuthandiza itakhala pamenepa ndipo mphatso ya uneneri itakhala pamenepa. Zonse mwa mphatso zili ndi malo ofanana chifukwa zonse ndi za Yesu! Kodi ichi chikupereka nzeru? (Ngati muli ndi makina a Kompuyuta, onani pa iwo. Aii at his feet.com / Jesus as Head kuti muone “chithunzi” cha ichi.

Tsopano, ngati mzimayi ali mubwalomu ali m'misonzi pa zakaleredwe ka ana ake, mphatso ya uphunzitsi ikhonza kuyankhula naye ndi kumuphunzitsa zokhudzana ndi zimene Paulo adanena mubuku la Tilo zokhudza azimayi. Mphatso ya chifundo ikhonza kupereka lingaliro la chifundo, mwina iye ali ndi ana a ang'ono kupereka panthawi imodzi ndipo akhonza kugawa zakuwawa za ichi. Mphatso imene ili ndi chidziwitso chauneneri ikhonza kuona mu mtima za *chifukwa* chimene mlongo uyu ali ndi mavuto ndi ana ake, ndi choncho. Tsopano, pomaliza, likhonza kumveradi moona lamulo lochokera kwa Mulungu, “pamene bvumbulutso libwera kwawachiwiri, siyani oyamba akhale pansu”. Allelluya!!!!!! (Mikuwo, ibwerenza)

Ali yense, ndiofunikira mofanana

Mu Akorinto oyamba 14, Mulungu adanananso “pamene mubwera pamodzi, abale, ndipo Mpingo uli pamodzi, lekani chili chonse chichitike mwakumanga kwa thupi la Khristu. Ali yense wa inu ali ndi inu la chilangizo salimo, bvumbulutso” Palibe bwana koma Yesu yekha! *“Musaitane*

munthu mtsogoleri, mbuye, mphunzitsi kapena m'busa. Nonse ndinu abale". Inu nonse muli ndi Yesu ndipo Iye ali chimodzi chimodzi mwa wina ali yense wa inu.

Mwachidziwikire pali kusiyana m'makhwimidwe, ndipo mphatso zina zili za "pachigulu" pamene mphatso zina zili zachete kapena zosaonekera onekera pa gulu. Koma, zonse zilipo ndipo zili ndi mwayi. Nthawi zina timafuna chifundo cha Yesu ndi nthawi zina timafuna chiphunzitso cha Yesu. Nthawi zina timafuna nyimbo za Yesu ndipo nthawi zina timafuna thandizo la Yesu kuti tithetse vuto. Koma zonse ndi za Yesu mofanana. Chonde werengani Akorinto oyamba 14:26-40.

Kodi mukhonza kuona kuti zimafunika kulimba mtima? Kodi mukhonza kuona kuti zimatengera chikhulupiriro ndi kumvera? Kodi mukhonza kuona kuti ichi chisinthwa moyo wanu ngati muyamba kukhala mu ichi? Kodi inu simungadzamangidwanso kumodzi ndi bedi! Mphatso yanu ndiyosiyana ndi yanga, koma yanu ndi chimodzimodzi ndi yanga. Ine ndikufuna mphatso yanu kwambiri monga inusno mufunitisa yanga.

Zinthu zina zofunika zimene zachitika mmoyo wanga zachitika chifukwa cha mwana wa zaka khumi ndi ziwiri ndi mphatso yake kukhudza moyo wanga. Azimayi kukhudza moyo wanga ndi ana kukhudza moyo wanga. Anthu okalamba kukhudza moyo wanga ndipo osati pa m'mawa, Lamulungu lokha ayi, koma tsiku liri lonse.

Ife tiri Ufumu wa ansembe tsiku liri lonse. Misonkhano ndi zongoonjezerapo ndithu. Mbali yokwana makumi asanu ndi anayi akukula kwathu imachokera mukukhala pamodzi, ndipo mwina mbali yokwana khumi limodzi chabe ndi m'mene imachokera mmisonkha. Ichi chitanthauza kuti muyenera kutuluka mnyumba zanu ndipo mulowe mnyumba za anthu ena. Inu munyamule madzi, kapena chakudya, kapena zovala popita kunyumba zawo. Pamene inu muona kuti ali ndi njala pamodzi ndi mwana, muyenera kuwatengera pambali ndikuyankhula nawo ndi kuyenda nawo. Pamene inu muona kuti ali ndi njala pamodzi ndi mwana, muyenera kuwatengera pambali ndikuyankhula nawo ndi kuyenda nawo. Pamene muona kudzitukumura mmoyo wawo, muyike dzanja lanu kuzungulira iwo ndi kuwafunsa iwo kuti sayenera kukhala oditukumura. Pamene inu muona kudzikonda mwa m'bale, inu muyenera

kuyika dzanja lanu mozungulira iye ndipo nati, "Chonde usakhalenso odzikonda ayi". Ife sitimangotseka maso athu kufikira msonkhano wina. Ife timakhala pakati pa moyo wa wina ndi mnzake tsiku liri lonse monga ansembe akuchita ntchito ya Mulungu, ndipo monga "zana la amai, abale ndi alongo" Ichinso ndi lamulo kuchokera kwa Mulungu mu Ahebri 3 ndiponso m'malemba ambiri.

Mwala wa madziko oyambandi "Kodi mkhristu ndi ndani? Kodi umembala wa Mpingo uti? Ngati inu muli ndi anthu amene siali otembenukira moona kwa Yesu mu Mpingo, ndiye kuti inu mudzakhala mapafupi pafupi ndi nkondo ndi ndewu imene simuyenera kukhala nayo. baibulo linena, "kuchokera kwa ang'ono kufikira kwa akulu, onse adzamudziwa iye." Pamene wina ali yense amene amadzitcha yekha membala *moonadi* ali m'chikondi ndi Yesu, pamakhala mtendere kwambiri - popanda nde, popanda mijedo. Ndipo pamakhala *chikondi chakuya pa wina ndi mnzake tsiku liri lonse*. Inu simungakhale membala woona wa Mpingo wa Yesu pokhapokha inu mutataya moyo wanu. Ndi Mkhristu yekha angakhale membala wa Mpingo. Ali yense ndi alendo chabe, koma iwo sakhala mamembala a Mpingo wa Yesu.

Ichi ndicho chenicheni cha zimene Baibulo linena. Ndipo "chotupitsa" chiyenera kuchotsedwa mu mktae, kapena ife sitimukonda Yesu monga m'mene tinenera. "Ngati mundikonda Ine, mudzamvera malamulo anga." Mpingo uli kulumikiza ndi kulimbikitsa ndi kuphunzitsa ndiponso kuteteza kwa amene adasambitsidwa mu Mwazi wa Yesu, atasankha kufa kwa iwo okha kuti akwatiwe ndi Mbuye, Yesu kwamuyaya. Ali yense amene sanapange chisankho, wakuyikiridwa umboni ndi moyo wawo ndi chosankha chawo, ndipo ndikuti ngati kapena ayi, "akonda kuwala" (Yoh 3, 1 Yoh 1), sayenera kudziyesa yekha Mkhristu kapena membala wa Thupi la Mkhristu. ichi ndi chimene Mulungu adanena.

Tanthauzo liri losne la "mpingo" ndi lopangidwa ndi munthu, ndipo "makomo a ndende" adzalaka chifanifani chotere. tayang'anani, inu mudzaona ichi mu mseu uli wonse mu mzinda ndi mzinda, fuko ndi fuko. Ichi simalingaliro a Mulungu, koma china chake chomwe chimangokwaniritsa mamvedwe a anthu, pamene akugwiritsa ntchito dzina la Yesu kuti achotsere nthumadzi zawo. Koma palibe kuchiritsidwa apo! Messiah yekha ndi amene amazungulira pamene Iye angasiyepo nyali!

Mwala wa madziko wachiwiri uli ndi chochita ndi mtsogoleri. Mzimu ndi Moyo wapano wa Khristu Owukistidwa, ndiye mtsogoleri yekha wathu. Dziko silidzandiona ine, koma *inu mudzandiona!* Mulingo wa Mzimu umene munthu ali nao, mphatso imene wina ali nayo, kukula ndi kuya kwenikweni kumene ubale wa moyo ndi Yesu wa Moyo umene ali nawo - icho ndiye matanthauziro a Baibulo a “Utsogoleri.”

Choonadi chachitatu: moyo wa tsiku ndi tsiku

Mwala wa madziko wa chitatu uli ndi chochita ndi moyo wathu wa tsiku ndi tsiku pamodzi ndipo ife tayankhulapo mochepe pa zaichi. Moyo wa tsiku ndi tsiku ulibe chochita ndi misonkhano imene timakhala nayo, koma koposa m'mene timakhalirana, ife timakhala tsiku liri lonse monga ansembe mumabanja ndipo ndi ana athu amene atizungulira ife, ndipo ndi magwiridwe ntchito ndi makhalidwe ofanana ndi anthu amene atizungulira ife? Kodi ife tikukhala tsiku liri lonse pa muyeso wa pa mtima ndi abale ndi alongo? Kodi ife “timasenzerana wina ndi mnzake chipyinjoni ndi kukwaniritsa Lamulo la Khristu? Kodi ife “timavomereza ndi kuululirana machimo athu wina ndi mnzake ndi kuti tichiritsidwe? Kodi ife “timakhala monga munthu m'modzi pa chikhulupiriro,” “molumikizana ndi kulukana pamodzi ndi munyewa yothandizira”, ndipo osavomereza chili chonse kupatula “Mpingo woota ndi “Thupi la Khristu”? Pamene pokha ndipamene mudzapeza chimene Yesu amatanthauza pakuti, Ndidzamanga Mpingo Wanga kuti makomo a ndende sadzaugonjetsa kapena kuyima!” Chinthu chili chonse ndi “nyumba yomangidwa pa mchenga” wa kunyalanyaza, kufunda, kusamvera, kusalumikizana. Ndipo udzabereka chipatso choyenerera, mwatsoka. Mulungu adati chili ndi kanthu kapena tanthauzo m'mene timangira!

Ine ndikuonetsani Malembo, amodzi ndipo asintha moyo wanu onse ngati mungamvere. Ngati inu mungachite malembo awa amodzi, inu mudzadabwitsidwa zam'mene zinthu zina izi zikuperekerana tanthauzo. Ichi ndi lamulo kuchokera kwa Yesu. Kodi mupanga ichi? Kodi mutero? Kodi inu mumukonda Iye? ichi chidzasintha moyo wanu onse kuti MUPANGE chimene Iye anena koposa kungogwirizana nacho kapena kungochiphunzira chabe kapena kungoyimba za icho kapena

kungokumnana pa zaichi. Tiyeni tiyang'ane pa ichi limodzi. malembowo ndi Ahebri 3:12-14

Penyani abale, kuti kapena ukakhale mwa wina wa inu, mtima woipa wosakhulupirikawakulekanandi Mulunguwamoyokomatundikudandaulilani nokha tsiku ndi tsiku pamen pachedwa lero, kuti angaumitsidwe wina wa inu ndi chenjelero la uchimo pakuti takhala ife olandilana ndi Kristu ngatitu tigwiritsa chiyambi chakutama kwathu kuchigwira kufikira chitsirizilo.

Dziwani chimene malembo awa akunena - ichi ndi chochokera kwa Mulungu. Mulungu wamphamvu zonse akunena kwa inu ndi ine kuti tiyenera tsiku liri lonse kuchenjezana wina ndi mnzake ndi kuthandizana wina ndi mnzake tsiku liri lonse. Mzimu Oyera udasankha kuti unene kuti “tsiku liri lonse”. Iwo siudanene kuti Lamulungu ndi la Chitatu liri lonse ayi. Iwo siudanene ngakhale kuti misonkhano mokha, iwo adati tikhale pa muyeso wa choonadi mo moyo wa wina ndi mnzake tsiku liri lonse. Ngati ena ali opezeka kapena akhonza kupezeka, ndipo inu simufuna kukhala nao kapena kukhudzidwa chifukwa cha moyo wanu, kapena kunyada, kapena kudzikonda, kapena chisankho chimene mungakhalire, Mulungu adati monga iye amvera. Inu mudzapusidwa mu kuganiza kuti mumadzi. Chimene chili choona pamene inu simudziwa. Icho ndi chimene malembo akunena mwatchuchutchu! Iye adangoti kuchipanga ichi, iye adati ngati simupanga ichi, chidzakuvulazani kwambiri. Ngati ine ndilibe m'bale ondiyankhula ine tsiku liri lonse zokhudza moyo wanga. Tsiku liri lonse ine ndidzasanduka olimba. Ine ndidzapusidwa. Inu mukhonza kunena kuti, “Koma ndimawerenga Baibulo tsiku liri lonse!” “Koma ndimapemphera tsiku liri lonse!” “Mkazi wanga ndi Mkristu ndipo ndimamuona iye tsiku liri lonse!” Icho sichimene Mulungu akunena, mukhonza kuwerenga baibulo ndi kupemphera tsiku liri lonse, koma ngati simufuna kukhala mu moyo wa wina ndi mnzake tsiku liri lonse, inu mudzakhala mukuwumila umilabe ndi kupusidwa pusidwabe. Mulungu adanena ichi mu Ahebri 3:12-14. Kodi mumakhulupirira baibulo? Kodi mumakhulupirira Mulungu?

Kodi adalemba baibulo ndani? Mulungu! Mulungu adanena kuti ife tiyenera kukhala mo moyo wa wina ndi mnzake tsiku liri lonse. Ngati muwona ine ndikudzikonda, mufunika kumbwera kwa ine ndi kunena, “m'bale, osakhala odzikonda. Ichi chipangitsa Yesu kukhumudwa.” Inu mukandiona ine ndikunyada, chonde bwerani ndi kundikumbutsa ine

kuti Mulungu amatsutsana ndi onyada. Ine sindifuna kuti Mulungu adane nane! Inu muyenera kuthandiza ine, chifukwa ine singingaone ichi nthawi zonse. Palibe amene angahe. *“Dandaulilani wina ndi mnzake, tsiku ndi tsiku kuti ali yense wa inu asadzimitsidwe mtim kapena kupisitsidwa”* Ichi ndi mbali yofunikira (ndipo siyimveredwa pafupi pafupi dziko lonse. Iyi ndi njira ya chifungulo imodzi yokhalira ansembe pogwirista ntchito mphatso, ndiponso *“akazembe a Khristu, monga ngati Mulungu amabweretsa chofuna chake kudzera mwa inu.”*

Choonadi Chachinayi: Misonkhano

Kwa zaka 1700, mudziko la chikristu mudali chosokonezo pa nkhanu yokhudza kuti Mkhristu ndi ndani mtsogoleri ndi ndani kodi moyo wa tsiku ndi tsiku uyenera kuoneka bwanji, maziko achinayi amakhudzana ndi misonkhano ya chikristu chakhala chosamveka kuchokera mu zaka 1700 ndipo kodi misonkhano iyenera kuoneka bwanji? Atate athu akufuna kubwezeretsa zinthu izi kwa inu mu moyo wanu tsopano. Monga ngati mau a Mulungu adatayidwira mu matsiku a Mfumu Yosiyu, ndipo choonandi chinakwiliridwa mu makhalidwe a ufumu ndi miyambo ya anthu, chonchonso lero Choonadi cha Mulungu, chakanidwa (koma chikadalibe mu Baibulo) koma chikhonza kumasula anthu mu ufulu. Mulungu adzasintha moyo wanu modabwitsa ndi kusinthanso ali yense ozungulira inu motsatira mwake. Ichi ndi choonadi champhamvu ndi cha mtengo wapadera. kaya muli anthu ambiri kapena ochepa m'mudzi wanuwo, monga Yonatani, bwenzi la pafupi la Davide adanenera, “Mulungu siali okanizidwa kupulumutsa kudzera mu ambiri kapena ochepa.” “Iye amene wagwirizitsidwa oyenera kuonetsa kukhulupirika” Ife tiyenera kukhala ndi kulimbika mtima kuti tipangepo china chake chokhudza ndi chilungamo chomwe chanyalanyazidwa kapena kusamveredwa ku mbuyo kwapitaku. Ndi iye mwini wake adzakhala m'busa wanu, linga lanu ndiponso mulonda wanu ngati mukhala molimba mwa Iye.

Ife tiyenera kukhala ndi kulimbika mtima, kukhala ndi misonkhano monga mafotokozedwe a Baibulo mu Akorinto Oyamba 14, “pamene mubwera pamodzi, abale, wina aliyense ali ndi mau achilangizo, salimo, bvumbulutso” Palibe wina olamulira kupatula Yesu yekha. Ife timasonkha pamodzi poganzira m'mene “tingasulirane win andi mnzake ku chikondi

ndi ntchito zabwino” (Ahebri 10:24-26). Ife tiyenera kuganzira ndi kupempherera pamene tingathandizirane wina ndi mnzake pamene tibwera pamodzi, ndipo wina ali yense wa ife atengepo udindo kukhala chonyamulira cha Mau a Mulungu ndi chikondi cha Mulungu. Ife tili ndi ali yense” kuganzira m'mene tingasulirane wina ndi mnzake ku chikondi ndi ntchito zabwino.” Ichi ndi icho chili mu Ahebri 10, chonde khalani otsimikizika ndipo yang'anani pa malemba amenewa! ichi ndi cha tonse a ife, ngakhale “mumisonkhano!”

Akorinto Oyamba 14 akunena kuti, “pamene bvumbulutso libwera kwa wachiwiri, siyani oyambayo akhale pansu.” Ichi ndi chimene baibulo linena. Nchifukwa chiyani sitichita chimene Baibulo limanena? Pasakhale “munthu wapadera” amene “mwachidziwikire” adziyembekezera kupanga chili chonse kupatula kumvetsera ndi kuyankha kwa Mulungu monga wina ali yense. Ngati wina wake abweretsa chiphunzitsa kuchokera kwa Yesu ndipo ena abwera ndi mau a chilangizo kapena salimo kapena bvumbulutso; ngati m'bale ameneyu kapena mlongo ameneyu akugawana nafe chinthu china, chomwe Yesu waonetsa kwa iye ndipo bvumbulutso labwera kwa wachiwiriyo, oyambayo akhale pansu - ngati tikumvera lamulo la Mulungu, koposa miyambo ya anthu. MOnga m'mene baibulo limanenera nthawi zonse.

Nchifukwa chiyani sitichita izi? Ndi chifukwa choti ife tatengera katundu olemetsa wa miyambo wochokera ku katolika ndi kuchokera ku “maprotestant” ndiponso ku “dzipembedzo” ndi makolo athu opembedza mafano. “Ansembe” kapena “abusa” kapena “audindo” ena onse ali kutsogolo, kuyankhula kwa wofunikira “pang'ono”, anthu osauka onse, anthu owonerera onse - atangokhala ndi kumamvera chabe. Ichi mwachidziwikire ndi machitidwe ndi miyambo imene Yesu adati amadana nayo, miyambo ya “Antikolatia” (kutanthauziridwa monga anthu amene ‘agonjetsa anthu ake’) Koma Mulungu eti adanena kale kuti zonse izi ziyenera kusintha chifukwa cha Iye ndi cha ife.

M'malo mwake Yesu adanena kwa “bwalo lokhalo momuzungulira Iye” kuti ali yense ali ndi liu la chilangizo, salimo, bvumbulutso. Ife tonse tili abale ndi alongo ndi zogowa zosiyana siyana othiridwa mwa Yesu ngati mwa m'modzi ndim'modzi pa chabwino chimodzi. Ndi chodabwitsa ndi chozizwitsa bwanji ichi! Iye AKUTIMASULA ife kuchokera ku

“miyambo yopanda kanthu yomwe tidalandila kuchokera ku makolo athu” pamodzi ndi utsogoleri wa mpingo ndi miyambo. Iye akutimasulira ife ku dziko “loopsya” la kumukhulupirira ndi kumukonda IYE monga zonse mu zonse wathu! Ndipo sikukhala chiwawa kumeneko, chifukwa Iye amadzitcha yekha, “Mulungu wa Mtendere” ndi “dongosolo” Ili ndi dongosolo lake chabe, osati kutengerapo mwai kwa Iye.

Madziko a kusintha

Ichi ndi chosiyana kuchokera pazimene tidazolowera kodi? Kodi tili nako kulimbika mtima kumanga m’njira ya Mulungu? Kodi ndizopatsa mantha? Kodi zikumveka mosekesa: Kodi ndi chosangalatsa? Anthu ena amene tili gawo la Mpingo tidali mbali ya amene adakhala ali a Khristu kwa zaka makumi awiri koma akadalidi makanda. Koma pamene adadziwa njira izi ndi kuyamba kugwira ntchito ngati ansembe! Adakula kukula kofunika zaa khumi pa chaka chimodzi. Alleluya! Ena adakhala “atsogoleri” m’mpingo imene idali ndi anthu mazana ndi zikwi. Iwo adapeza kuti mu uzimu akadali makanda! Iwo amaganiza kuti ndi atsogoleri, koma adapeza kuti ana ndi amai ambiri adali a uzimu koposa iwe. Iwo amayenera kukula kuchokera kukhala khanda, ndipo adakula! Zonse izi ndi zopatsa mantha kwambiri, komanso ndo zosangalatsa kwambiri.

Ngati muika choonadi ichi chimene chakhala mu Baibulo nthawi zonse mudzakhala odabwa mmene mudzakhali pafupi ndi Yesu zaka ziwiri kuchokera pano. “Khalani limodzi tsiku ndi tsiku”. Monga pamodzi ndi ana anu, mabanja anu ndi kuntchito kwanu tsiku lililonse. Pitani kumeneko! Ndipo chokani kumalo kumene muli ndikuchita zimene simunachitepo inde ndikulankhulala ndi inu, chitani izi kwa Yesu. Lankhulani mau ake monga mau a Mulungu kwa miyoyo yanu mwachitsanzo kundanani munzeru yabwino tsiku lonse. Pamene mubwera limodzi abale wina ali ndi kanthu nyimbo kapena vumbulutso. Pamene vumbulutso libwera kwa wachiwiri, woyambayo akhale pansu. Mukachita izi mudzapeza kuti ena sakukonda Yesu ngati mmene mumaganizira. Ndipo ena amene mumawaganizira kuti ndiwofooka adzakhala amphamvu ndi a nzeru kusiyana ndi mmene mumaganizira. Njira ya Mulungu imaonetsera zinthu zopanda pake ndikukhazikitsa zofooka kukhala zamphamvu. Atamandike Mulungu!

Chuma ichi chapatsidwa kwa inu muchigwiritse ntchito mokomera Yesu miyala imeneyi ndiye maziko mueyenera kuonetsera kuti Khristu ndi ndani monga Yesu ananenera. Mueyenera kudziwa utsogoleri umakhala otani, khalani miyoyo yanu tsiku lonse, pamodzi limbikitsanani wina ndi mnzake manganani wina ndi mnzake, thandizanani kukula kukula ndi kukonda Yesu kopitirira masana ano ndi madzaulo ano. Bwerani ndikukumanana pamodzi mozungulira Mfumu Yesu.

Ngati mukonda Yesu ndikumanga njira yoeyenera, malinga andende sadzapambana ayi, uchimo udzawonongedwa, kufooka ndi matenda kudzachiritsidwa. Uchimo udzakhulukidwa. Kukoma mtima kudzatitengera kukulapa. Ubale udzamangindwanso ndi kukonzedwanso mopitirira mmene mumaganizira mumaloto anu abwino. Muzakhala owala monga nyenyezi zakumwamba kuonetsera ubwino wa Mulungu. Ndi mkwatibwi, mpingo wake adzadzikonzeke retsa ndipo konzeke rani pamene mkwati abwera. Amen

Kubowoleza Kwa Ulemerero

October 3, 1999, Salima, Africa.

Ngati tikumanga chomanga mwani nyumba uzakhumbila katundu; chochekela nyundo, misomali chomangila, chonenetsa mu nyumba ya Mulungu. Pamakhala katundu wina wofunikila. Ngakhale zili choncho mpingo onenetsa wa Yesu siukhuzidwa mu misonkhano, nthawi zina misonkhano ndi yofunika monga zina zogwilira ntchito, ngati timayimba pamodzi mwa Yesu, pamakhala zinthu zina zimene timaphunzira kuchokera kwa abale ndi alongo. Ngati unapitako ku bwalo la milandu ndi kulakhulapo ndi iwo ngati amawona nthawi ya pa mkono, ndi kupitsa mu thumba mwina kulankhula ndi ena. Oweruza safuna choncho ngati ukuyankhula ndi iyeyo utha kugona kusinza kapenanso kungozisiya choncho kapena kusayankhulapo kanthu, akhoza kunena kwa inu. “tulukani mupite mukachite zenizeni. Mukakonzeka kumvera ineyo, mutha kubweranso. Muntha kuchoka pokhapokha mutazikonzeke latsatso.

Mulungu chimodzimodzi. Tikamayimbira Yesu, ngati timuyimbira mu choonadi Yesu, mitima yathu yimalumikizana naye. Maonekedwe a nkhope yanu, kapenyedwe ka maso anu, mphamvu ya liu lanu kuthekera kwa kukhalabe mumaonekedwe izi ndi zinthu zonse zimene zili mbali ya chiyanjano ndi mfumu ya mafumu. Msonkhano umakhala waphindu, ndipo tsopano ndikupatsani chida misonkhano yimakhala ndi gawo lochepa kusiya ndi moyo wathu mwa Yesu. Momwe tingathandizire abale ndi alongo monga a nsembe. Ngati pali munthu wina wayima pafupi ndi inu pamene mukuyimba pamodzi iye ndi kutaya chidwi mukuyimba, ndi chizindikile kuti akufuna kuthandizidwa. Kuti bvuto lake ndi chiyani. Mumayimbidwe osangalatsa. Kuyimba ndi kulumikizana – kuyimbila mfumu ya ulemelero.

Kwa nthawi zimalankhulidwa mu nyimbo yina, za mubuku na nyimbo za uzimu ngati ndimalankhula ndi Yoswa ndi kusiya mwina kupenya mu mwamba kuona kusagwilizana ndi iye. Ndi pamene pakhala chida chothandiza kumanga nyumba ya Mulungu. Momwe Paulo anenera, “mukangano wa aliyense kuzionetsera kukwanilitsa, mwina kuziyeretsa mwa khristu. Wansembe mwina ansembeyo ayenera kukanganira kuwoneka kwa aliyense moyera mwina kukwanilitsa mwa Khristu. Iyi ndi

ntchito yanu mu nyumba ya Mulungu. Osati kukhala ndi kumvela, osati kuyimba kokha, koma baibolo likuti “tiyanganire kwa kuzionetsera mwa aliyense kulungama mwa Khristu”

Ngati wina mwa inuyo ali ndi uchimo mwa mtima wosakhulupira.nde pali zida kukuthandizani kuchita ichi. Ngati muli pamozi ndi aliyense kuimba, mutha kuwona nkhope zina, kuyera? Mutha kugwira chokhacho muona kumbuyo kwa mutu wawo. Koma tsopano tili banja ndipo tingaonane wina ndi mzake ngati ndili kuimba nyimbo kwa inu ndingathe kuona kwa inu ndi kumwetulira ndi kuimba nyimbo ngati monga ndilankhula ndi inu. Ngati ndili ndi mtima wanga ndi kuyimba ngati kuti ndili kulankhula ndi wina wake amene ndili ine. Ngati ndili kuyimba koma osakhudwidwa ndikugwedeza mutu wanga osalabadira ndi kumangoyang’ana uku ndi uko – ndiye uyenera kufunsa iwe kuti zili bwanji ine ndi ubale wanga ndi Yesu. Chodziwika ndi choti pali mabvuto amene ali ndi mgwilizano wanga ndi Yesu ngati ndili kulingalira zina pamene ndili kulankhula ndi iye.

Baibulo limati aKristu wowona monga omwa mkaka, amafuna mkaka wa uzimu wa mau a Mulungu Akristo wowona amafuna chiyanjano ndi Yesu monga mmene makanda afunira mkaka. Yesu anati kuti amene ali ake chilakolako cha nyumba ta Atate chimatidya monga moto kunyeketsa chitsulo. Tili ndi moto mu mafupa amane sangazimitsidwe. Ndipo ngati muona wina amene ali chitsulo chonyowa ndipo moto sikunyeketsa, monga utsi, ndiye pafupi ka kuwathandiza iwowo.

Chimodzi cha zida zothandizira kumanga nyumba ya Mulungu zimene zingakupatseni ngati chida chabwino ndi kukweza miyoyo yathu kwa Mulungu. Ngati mungaone anthu amene Sali okhudwidwa kapena kuzichotsera kapena osasalimira kapena kukhala ongosangalala ndi za Yesu. Ganizani za izi ndipo pemphelani za iwo. Mwina pitani ku nyumba zawo tsiku lililonse. Afunzeni mmene ali kumvera, ndipo amene ali kumvera zinthuzo. Nenani “ndaona kuti muli kulalikira naye Yesu ndipo simulinso kuonetsera chikondi kwa iye. Simunali kuika mtima wanu kwa zinthu izi. ndipo ndili odabwa ngati muli ndi mkwiyo pa zinthu zina. Ndi chiti chimene chilli chopambana pa moyo wanu koposa Yesu? Kodi mwilankhura mu nthawi yabwino ndi Yesu mukupemphera kwanu kwapadera? Kapena muli kupezeka chabe mu msonkhano pamene chiyangano ndi iye. Sichili bwino? Choncho ichi ndi njira imodzi imene mungathandizilane nonse pamodzi

kukhala mwa Yesu ndikukhala tcheru ndi anthu nonse pamodzi pa malo amodzi. Iyi ndi nira imodzi imene ife ansembe osati ongoonera chabe.

Zimene anthu oipa amanena

Panali munthu oipa tsiku lina otchedwa Kaini mukumbuka Kaini, mwana wa Adamu. Anali oip china chimene amanena ndi choti. Sali osamalira mbale wake. Anthu oipa matero ndithu ife ndife osunga mbale wathu. Timakondana wina ndi mzake kuchokera mu mtima wakuya.

Timalimbana kudzipeleka wina ndi nzake molungama kapena watunthu mwa Yesu. Tidali mu zowawa mkubadwa kwithu mpaka Yesu wakhalamo mwa abale ndi alongo. Izi ndi zimene tinena kwa inu. Nchifukwa chake tabwera kuchokera ma dela onse osiyana a dziko kudzakuwuzani zinthu izi;

Tabwera kudzayetsesa kudzalengeza kwa inu za chilungamo mwa Yesu. Ndipo muyenera kuchita ichi kwa wina ndi nzake mchilungamo mwa Yesu. Si inu ndi chiyanjano chanu ndi Mulungu. Ndife ambiri koma ndife amodzi mwa Yesu, bukhu loyera likutero. Ngati chala chanu chikudwala kapena chilli ndi vuto lina lake, mumayamba kumva mutu kupweteka, mumamva kuzizira – thupi lanu lonse limaphwanyanya. Ndizowonanso ndi thupi la Yesu, ngati mmodzi wa ife wavulala mu uzimu tonse timakhudwidwa mu uzimu.

Ndife anthu osunga abale, ngati muwona wina wake amene ali ndi vuto ndi chiyanjano chake ndi Mulungu mkupembedza kapena mukaleledwe ka ana kapena munjila ina, tiyenela kuthandizana wina ndi nzake. Ife mmene tili ambiri ndife amodzi. Ndife amodzi wina ndi mzake kupyola mtunda, kupyolanso zaka. Ndife amodzi ndipo timafanana wina ndi nzake. Ndipo timakondana pothandizana wina ndi mzake kukula mu uzimu.

Ndiye chida mmanja mawanu pakumanga kachisi wa Mulungu ndi kumvetetsana wina ndi mzake – tikakhala malo amodzi. Ndipo ngati muwona wina wake safuna kulowa mwa Mulungu ndi mwa anthu ena.

(ali pano potha chabe nthawi) ndipo ndiowonangedwa, ndiye muyenda kulowa mmiyoyo mwawo ndi mmakomo mwawa ndikuwatenga iwo ndi dzanja ndi kuwathandiza kumukonda Yesu kwambiri. Ndinu woyanganila

mbale wanu. Tiyenela kuthandizana wina ndi mnzake. Timvetetsane wina ndi mzake.

Pamene tinayimba nyimbo yotsiliza kodi mudalumikizana ndi mtima wa Mulungu? Ndipo kodi mudayamba mwayangana malo okuzungulilani ngati alipo akuvutika? Ena amene alibe chidwa? Ena amane awukira Mulungu ndipo akufuna machilitso enei eni?

Ena amene ndi ofowoka ndiye sakumvetsetsa bwino, zilipo zina pang'ono mwa zinthu zimenezi. Chifukwa takhala womangidwa ntahwi yayitali, sitinathe kupeleka chidwi ku zinthu izi. ino ndi nthawi imene tiyenela kukula ndi kutengapo gawo mu nyumba ya Mulungu. Tsopano zili m'mznja mwathu pamodzi kutumikila zolinga za Mulungu mu mbadwo wathu. Amen?

Pamene zili zowona kuti zinthu izi zingathe kudzetsa kugawikana, zitha kuwonetsa poyela za mkati mwathu zobisika pamene tinkavina ndi kulambila. Anthu ena amakonda kuwala ndipo ena amadana ndi kuwala. Tsono kukhala koteleku kudzetsa kugawinikana chifukwa ena amakukonda kuwala ndipo ena amadana ndi kuwala. Yesuanati sindinadze kubweretsa Mtendere koma lupanga. Nthawi zina zitha kugawanitsa anthu ambanja wina ndi mzake.

Uthenga Wabwino

Ife tomwe tili ndi mipatuko. Muyenda munjila kumene mwalowela, muwona mtundu yonse ya kugawikana. Mpingo wa Yesu, Nazarene, Lutheran, katolika. Pali kugawinikana kwakukulu. Koma, pano pali uthenga wabwino. Ngati mukhala ngati ufumu wa Mulungu monga chipembedzo chimodzi, ngati mulalika za Yesu lalikani osati chipembedzo, ngati mufuma muthandiza anthu ena – kukonda Yesu kuti tichotse chimo, ndi kukhala abwenzi a Babasiti. Alutherani ndi ena otere, aliyense adzayamba kusiya zizindikiro, ndi zimene zidzachitika muno mu Salima? Pamene aliyense adzabwera ndi kudziwa mabvumbulutso ndi kumamvera iwo uku ndi uku mu misewu. Sipadzakhalanso kusiyana. Koma kusiyana kudzakhala pakati pa ofuna kukonda Yesu ndi amene safuna kukonda Yesu ndi kumvera Yesu. Mmallo mwa zopusa zimene zili zimene tili nazo tsopano kusiyana kudzakhala mu kukondana ndi kumvera ndi osati miyambo

yathu, ndipo Yesu adzakhala ndi umboni mu mzinda uno mu umodzi umene sunalipo ndi kale lomwe. Ndi chifukwa chake ndi chofunika kuti mumange mu njira imene tili kulankhura kwa inu lero fikirani miyoyo wanu kwa okhulupilira mu mzinda uno ndi kuthandiza kumanga mu njira imeneyi. Potere sipadzakhalanso kusiyana ndi mayina kusiyana kwa amene akufuna kukonda ndi kumvera Yesu ndi amene angofuna kusewera ndi “chipembedzo” siuthenga wabwino kodi?

Ngati tingaphunzire kukhala motere, miyoyo wa anthu idzasintha. Anthu adzaoneka monga Yesu. Padzakhala wina amene muli kumusamalira kwambiri ndi inu ndi ena onse pamodzi mudzalimbika kuti mumuonetsere watunthu kwa Kristo. Mudzamuona munthu ameneyu kupanga chiganizo chomvera Yesu ndikuona kusinthika mu moyo wa munthuyo. Kodi mukudziwa kuti mudzakwanitsa ngati muli nonse pamodzi ndi abale ndi alongo? Mudzaimba mokweza chifukwa mudzakhala mukuyamika Mulungu pazimene ali kuchita. Simudzaganizo inde, ndiyimbe mokweza ine ndine wa “Pentekositi” mudzayamba kuganiza kuti Yesu wapanga zinthu zopambana moyo wanu. “ndifuna kumuyamika iye.” Zimene tikulankhula lero lino pano – zimene miyoyo wa anthu idzasintha, mmene Yesu adzabwera kwa anthu ake. Ndizimene tidzaimbira nyimbo! Ndizimene tizayamika nazo Mulungu koposa!

Satana adzaonongedwa mu miyoyo yathu ndi zimene tidzayamike nazo Mulungu koposa!

Ndikukuuzani kuti pamene tinayamba kuyenda mu zinthu izi zaka khumi ndi zisanu zapitazo zinali zomvetsa mantha ndi zolimbikitsa kodi muli ndi mantha otere?

Mukuoneka olimbika koposa mmene ine ndinalili chifukwa zinali zobvuta kwa ine poyamba. Koma patapita zaka khumi ndi zisanu ndi zikwi za anthu mu dziko lonse lapansi amene anayamba kuyenda mi zinthu zimenezi ndi zabwino ndipo mantha anatha, choncho Mulungu adzatsinjiliza mu nzeru ndi chikondi pamene mupita patsogolo mu zinthu izi. adzatipatsa zosowa zathu monga mwa kuchulukwa mu ulemmero wake. Zizakhala bwino, adzakhala Atate kwa ife. Adzakhala mphunzitsi ndi otikonda miyoyo yathu. Ndipo tidzapitilira mu njira zobvuta zambiri. Yesu adzapambana mu msewu ndi mzinda yonse uno, adzapambana mu mitima yathu. Pamene

mantha, kuzikonda, ndi kunyada zimakhala. Adzatichapa ife ndikumanga ife odzadza ndi afulu mu njira pa zimene sitingafunse kapena kuganizira. Zinthu izi ndi zoono ndipo mudzakhala mu zimenezi ngati mudzatsegule moyo wanu ndi kupita patsogolo.

Pamene Yoshua anapita mu dziko lalonjezo Mulungu anati “osachite mantha” ndipo pamene ansembe anayamba kulowa mu mtsinje kunali kobvuta kwa iwo pang’ono, Baibulo limati sanayendepo njira imeneyi mbuyomu ndipo Mulungu anati “chabwino” ndidzakhala nawe” ndipo zinthu izi ndi zoono kwa inunso. Osati pa malo pano pokha ndi malo ozunguliriz mzinda uno. Mulungu adzakhala ndi inu pamane mudzapita patsogolo ndi mau ake. Khalani ndi mphamvu ndi kulimbika! Mulungu akuti “monga ndinali ndi Mose monganso ndinakhala ndi iwe mu nthawi yapitayi choncho ndidzakhala ndi iwenso monga mmene uli kupitira chitsogolo osaopa ai”

Abale ena atalankhulanso popeleka miyoyo yawo.

Abale ndi alongo mwaona zimene zikuchitika pano lero? Tayamba kuona ufumu wa Ansembe. Pamene bvumbulutso libwera kwa wina okhalapo. Woyambayo akhale pansu. Ndipo pamene bvumbulutso lafika kwa winanso ndi winanso!! (kunali kukuwa pokweza mau)

Mipando Isanu

Lachiwiri Masana Salima, Malawi October 5, 1999

Mwachisomo cha Mulungu, ndifuna ndiyikize kwa inu zida zina za kuvetsetsa ndi kuzindikira makhalidwe a anthu. Tingoyezera, kwa kanyengo kamene tili nako pano ife, mipando isanu. Ndipo akukhala mipando isanu imeneyi ndi anthu asanu kuyimirira mitundu isanu ya anthu amene inu mwachidziwikire mukumane nayo pa ulendo wanu padziko lapansi.

Mipando iwiri yoyamba

Mu mpando oyamba, tili ndi osakhulupirira kapena wamafano wina wake sakhudzidwa ndi zotsata Yesu ndi pang’ono pomwe. Mwina munthu ameneyu ndi msilamu kapena Mhindu. Munthu uyu samazitcha kukhala Mkhristu .

Mu mpando wa chiwiri, ngakhale, tili ndi munthu amene amazitcha kuti amasatira Yesu, koma munthu uyu samvera Yesu. Pa misonkhano, munthu uyu amaoneka ngati okonda

Yesu, koma iye samkonda zenizeni chifukwa samvera iye. Mu Mateyo 7, Yesu adati padzakhala ambiri amene adzanene “*Ambuye, ambuye* padzakhala ambiri amene adzagwire nchitho yotamandika mu dzina lake, koma ku amene iye adzanena “Ndichokereni ine, ine sindikudziwani inu”

Aliyense akudziwa kuti munthu wa mpando woyamba sali owomboledwa chifukwa munthuyu sazitcha ngakhale pang’ono kuti amasatira Yesu. Iye timadziwa kuti pokhapokha ngati uli ndi mwana, siungakhale ndi Atate. Pokhapokha ngati ukhulupira mumtima wako kuti mulungu adaukitsa Yesu kwa kufa, Mwazi siudzatsuka tchimo lako. Munthu uyu sangapulumsidwe chifukwa iye sakhulupirira mwa Yesu. Mwazi wa Yesu siutsuka machimo amunthu otereyo. Kufikira munthu wa mpando woyamba uyu atadzipereka kwa Yesu, iye sangapulumsidwe. Iye akhoza katengedwa kukhala munthu wodabwitsa ndi tate wa bwino ndiponso wachitho wabwino, koma iye sangapulumsidwe kopanda kuyeletsedwa ndi mwazi wa Yesu.

Kumbali yinayi, munthu wa mpando wachiwiri anena “ine ndine mkhristu” koma makhalidwe amunthu ameneyo ndi oyipa, ngakhale kuti munthu uyu akhoza kupanga nchitho zabwino zowoneka mzina la Yesu. Mu uthenga wabwino wa Luka, Yesu adati kuti pa tsiku la chiwerunzo, anthu ngati uyu adzanena, “Yesu, mudaphunzitsa makwalala athu. Mudadya magome athu. Ife tidapanga zozizitswa mu dzina lanu. Tidapereka chuma chatu kwa osauka”, koma Yesu amanena kwa anthu awa mu mateyo 7:21. “inu simudamvere ine inu simudapange funiro la atate. ine sindidakuziweni inu. Yesu akuonetsa apa kuti anthu ambiri amene mazichtha a khristu ndi mpakaso amapanga nchitho za mphavu mun dzina lake ali munjira ya chikulu yomwe imasogolera ku chionongeko. Anthu awa amanamizira kukhala a khristu, amanamiziran kuti ali ndi mamembala a mpingo, koma mzenizeni saali choncho.

Munthu wa mpando woyamba siali opulumusidwa chifukwa cha kusakhulupirira. Munthu mumpando wachiwiriwo siali opulumusidwa chifukwa chakusamvera, kumene Baibulo limanena kuti ndi osakhulupiriranso.

Mipando itatu inayo

Tsopano anthu amipando atatu yotsaklayo ayimirira choonadi. Otsatira a Yesu ogulidwa ndi mwazi. Atatu awa ndiwo a khristu koma ndifuna kuunika kuti pasakhale chisokonezo ndi munthu wampando wachiwiriwo.

Muli ndime zogwirizika kwambiri mu Yohane oyamba 2 imene imaonetsera ndikuzindikiritsa anthu amenewa amene tili nawo mmipando itatu yomalizayi. Yohane adati “Ndikulembera kwa inu ana ang’ono, azibambo ndi kwa inu achinyamata” Tsopano mmganizo athu a nthawi zonse mudongosolo la zinthu ndi ana ang’ono, achinyamata ndiponso azibambo sichoncho. Koma Mulungu akupereka dongosolo ili, “ana, abambo, achinyamata”

Ana, abambo, achinyamata awa ndi anthu opulumusidwa. Awa ndi anthu amene amakhulupirira kuti Yesu ndi mwana wa mulungu, ndipo machimo awo ndi wokhululukiridwa ndipo ndi osambitsidwa ndi mwazi wake. Mpando wachitatu uyimira ana, mpando wachinayi uyimira abambo ndipo mpando wachisanu uyimira achimata. Inu mukhoza kuganizira iwo monga

makanda , anthu okhwima kapena akuthekera ndipo kenako chinthu chimene ndikufuna kuti ndionetsere bwinobwino ndi chakuti nthawi zina makhalidwe a ana ngakhale kuti iwo ali opulumutsidwa, amaoneka ngati makhalidwe a anthu asapulumutsidwa (ngati munthu wa mpando wa chiwiri). Koma munthu wa mpando wa chitatu (Mwana weniweni) ndi osambitsidwa ndi mwazi wa Yesu. Munthu uyu wa mpando wa chiwiri akhoza kuzitcha kuti anasambitsidwa m’mwazi wa Yesu. Munthu ameneyo akhoza ngakhale kuimba nyimbo zokhudza Mwazi Yesu kuwapulumutsa iwo , koma chifukwa munthu uyu akhoza pang’ono ndi pang’ono

Kupita mpaka kupandukako kwa Yesu, munthu uyu siotsatira wa Yesu weniweni. Aliyense amene amazitcha kuti ali mwa iye , ayenera kuyenda m’mene Yesu adayendera. Aliyense amene sadzamvera kwa Yesu adzadulidwa kuchokera pakati pa anthu “Aliyense amene ali ndi chiyembezo ichi adziyeretsa yekha monga iye ali woyera. Palibe amene adabadwadi kwa mulungu amene adzapitilira kuchimwa chifukwa mbewu ya mulungu imakhallira mwa iye, iye sangapitirire kuchimwa chifukwa iye ali obadwa mwa mulungu.

Njakata ya mpando wachiwiri/Mpando wachitatu

Nthawi zina khalidwe la munthu wa mpando wachiwiri likhonza ngakhale lukhalako labwino kuposa khalidwe la munthu wa mpando wachitatu. Koma pali chinthu china chimene muyenera kumvetsetsa chokhudzana ndi uthenga wabwino wa Yesu. Munthu wampando wachitatu ndi kufunafuna kuyeretsedwa mu Mwazi wake. Mu Aefeso I ndi Agalatiya 3 Mulungu adati kuti pamene munthu akhulupirira mu mtima mwake (osati mmutu mwake) mwa Yesu khristu kuti amapatsa munthu ameneyo MphatsoYa Mzimu oyera kuti ikhale mkati mwake. Mzimu oyera umapatsidwa kwa aliyense amene akhulupirira moona ndipo akhulupirira mwa Yesu kuchokera mu mtima

Tsopano muli mu njakata. Ngati inu mukungoweruza kudzera mumakhalidwe , ungadziwe bwanji mmene ungachitire? Nanga bwanji utakumana ndi mkhristu wa chimwana amene ali ndikhalidwe losasangalatsa , ndipo muli ndi osakhulupirira amene amazitcha m’khristu koma pa zonse mungaone , mungaone mwina ali ndi khalidwe la bwinoko?

Chabwino kodi alipo wina amene adapulumutsidwa ku machimo chifukwa cha khalidwe la bwino? Kodi ichi ndicho uthenga wa bwino wa Yesu? Kodi uthenga wa bwino ndiwoti kupulumusidwa ndi makhalidwe athu abwino? Ayi sichoncho! Ife tapulumutsidwa ndi mwazi wa Yesu. Ife tapulumutsidwa ku machimo athu ambuyomu, ndipo tapulumutsidwa ku machimo obwera mtsogolo ndi Mwazi wa Yesu khristu.

Tsono kenako, nchifukwa kumanenedwa mbaibulo mbuku la Agalatiya kuti aliyense amene akhala ngati wochimwa sadzalowa mu ufumu wa mulungu? Ichi chikumveka kuti chipulumutso chatu ndichokhuzidwa ndi makhalidwe athu. Koma ife timadziwa kuti ichi sichingakhale choona ife tinapulumutsidwa ndi mwazi wa Yesu, osati makhalidwe athu. Tsono keneko nchifukwa chayani Baibulo limanena kuti aliyense akhala mmachimo sangalowe mu ufumu wa mulungu ndipo sadzapita kumwamba? Nchifukwa chiyani Yesu amati, “Nkhosa ndi amene achita chifuniro changa ndi kundimvera ine, ndipo Mbuzi ndi amene sandimvera ine? Yesu adati nkhoa zikupita kumwamba ndipo Mbuzi zikupita ku Gahena. Ndipo Yesu adati mudzidziwa nkhoa kudzera mu zi ntchito zawo. Ichi chikumveka ngati tinapulumutsidwa ndi makhalidwe athu. Koma ife tidziwa izi sizoon.

Kuthana ndi njakata

Kodi uthenga ndi chiyani apa? Kodi timamveka bwanji mbali iyi ya uthenga wabwino? Chabwino ichi ndi chisisi cha uthenga wa bwino wa Yesu. Aliwonse amene amapereka mitima yawo kwa Yesu ndipo atembenuka ku machimo ndikusiya zammbuyo mwawo amapatsidwa Mphatso ya mzimu oyera. Ife timawerenga mu buku la Yohane Oyamba kuti pali zizindikiro zambiri zimene mzimu wakukhala mkati umaoneka ngati moyo wa umunthu. Pali ambiri amene adzanena “Ambuye, Ambuye” koma adzamva Yesu akuti” sindikukudziwani ndi pang’ono pomwe” Tsono ife tikudziwa kuti munthu saali mkhristu chifukwa choti munthuyo amazitcha kukhala kapena amachita zinthu zooneka zodabwitsa mzina laYesu.

Buku la Yohane Oyamba lidalembedwa mu zaka zokwana makumi asanu ndi limodzi patangotha pentekosti. Mtumwi Yohane mwina adali ndi zaka makumi asanu ndi atatu ndi mphambu zisanu kapena makumi asanu ndi anayi. Yohane adali ndi zaka zambiri kuti aganize kapena kuti

apemphere zokhudzana ndi chikhristu chimaonekera. Pa nthawi imeneyi, zaka makumi asanu ndi limodzi patatha masiku a Pentekosti, padali anthu ambiri omwe adali atakula mpingo. Padali makanda atsopano obadwa amene adakula ndipo adali ndi ana awo nawonso pa nthawi imaeneyi. Tsono pamene anthu amene adakula akunena mau olondola chifukwa makolo awo adanena mawu olondola pa nthawi imeneyi, padali anthu ambiri amene “adakulira mumpingo” ndipo mwachoncho adadziwa nyimbo ndi akhonza kuomba mmanja ndi kuimba ndi kunena mawu onse olondola. Koma Yohane adadziwa kuti ngakhale ana akhonza kuoneka a khristu, iwo akhonza kukhala asanadzipereke miyoyo yawo moonadi kwa Yesu. Munthu si mu khristu chifukwa choti mmalingaliro amakhululupirira zinthu zoon. Munthu, kutengera pa Yesu, sim khristu mkhristu chifukwa chopanga zinthu zozizwa mu dzina lake. Padzakhala anthu pa tsikulo, amene adapanga zozizwa mu dzina lake, ndipo iye adzawauza iwo “Ndichokereni ine kunka kunja ku mdima. Ine sindidadziweni inu.”

Gawo la mzimu woyera

Monga ndidanena buku la Yohane Oyamba adalembedwa zaka makumi asanu ndi limodzi patatha pentekosti. Yohane amayankha ambiri mwa mafunso amenewa amene mwa chidziwikire iye adayenera kukumana nawonso. Yohane adalemba zinthu zosiyana zambiri mu buku la Yohane Oyamba zimafotokoza chimene mkhristu weniweni amaoneka ngati. Nthawi ndi nthawi iye amalongsola chimene chimaoneka ngati wina wake ali ndi umboni wa Mphatso yakukhala mkati ya mzimu oyera. Baibulo limati kuti aliyense amene ali mkhristu oona ali ndi gawo kapena gawo la malipiro otchedwa mzimu Oyera.

Pamene munthu akugula nyumba kapena galimoto, nthawi zina amapereka mbali ya malipiro kapena malipiro oyamba gawo limenelo. Kapena mbali ya malipiro oyambawo amakhala ngati chikole kuti malipiro onse adzabwera. Baibulo limati kuti Mulungu, monga mbali ya malipiro, adapereka mzimu woyera kwa aliyense okhulupirira. Ichi ndi chitsimikizo kwa ife kuti ife tidzatenga moyo kwamyaya. Ngati wina wake akusoweka mbali ya malipiro imeneyi, gawo la Mzimu woyera, ndi chidzindikiro kuti pakhala popanda pangano kapena mgwirizano pati pa munthuyo ndi Yesu.

Ichi ndi chifukwa chake Yohane, mtumwi adati kuti kusiyana kwa Mkhristu ndi osakhulupirira sikulapa kwa ngati amapanga zozizwitsa, kapena ngati amakhulupirira zinthu zolonda, koma ngati ali ndi mzimu woyera . Ndipo chimaoneka bwanji pamene munthu moonadi ali ndi mzimu woyera ? Kodi ndikupanga zozizwa ? Kodi ndikuyimba ndi kukhala nawo misonkhano ? Ayi izi siziwonetsera zimene zimathandiza ife kumvetsetsa amene ali ndi mzimu ndiponso amene alibe . Munthu wampando wachitatuwo , amene ali mwana wachikhulupiriro, akhoza akhonza kukhala kuti adanzipereka kwa Yesu kuchokera mtima, koma akhoza kuonetsa khalidwe loipa nthawi zina.

Ena anakonda kuwala

Yohane ndi Yesu anapereka kwa ife yesero lofinika kwambiri kutithandiza ife kutolapo kanthu pa chisokonezo ichi. Yesu anachiyika choncho, *“Ena anakonda kuwala ndipo ena amadana ndi kuwala”* (Yohane 3) Yohane adati *“Ngati ife tikhonza kupitiriza kuchimwa, ndiye kuti Sitidziwa . Mulungu, ndipo ife tawonetsera kuti ife tilibe Mzimu Oyera.”* (1 Yohane 1:4).

Yesu adati *“Ena anakonda kuwala, ndipo ena anadana ndi kuwala.”* Makhaliidwe a munthu uyu opulumutsidwa akhoza kusakhala wabwino nthawi zina, koma chifukwa munthu uyu ali ndi Mzimu Oyera mmoyo wake, munthu uyu adzakonda kuwala ndi choonadi. Monga khanda lobadwa kumene, munthu uyu adzakakamira pa mkaka wa uzimu wa Mau. Pamene mudzayandikira munthu uyu ndi kunena , *“khalidwe lako ku nchito, kapena ndi mkazi wako ndi losakhutitsa m’bale. Kodi ukudziwa kuti pamene uchita zinthu izi wukuwawitsa mtima anthu ambiri kuphatikizirapo Yesu?”* Munthu wa mpando wa chitatu uyu akhoza kuyamba kulira ndipo nati *“ukunena zoono. Ndikudziwa kuti ukunena chilungano. Mu mtima mwanga ndine odandaula mmene ndawachitira akazi anga. Zikomo pakubwera kwako kudzandiuza . Ine ndikufuna iwe undiuzze zinthu zimenezi. Ndikufuna thandizo lako.”* Uwu ndi umboni waukulu kuti munthu uyu ali ndi Mzimu Oyera ndipo ali oomboledwa.

Mwina makhalidwe a munthu uyu siabwino ku nyumba kapena kunchito poyamba, koma Baibolo likunena kuti ngati wina ndi opulumutsidwa, Mzimu Oyera udzadzionetsera Okha ndi chikondi pakuwala ndi

choonadi. Munthu uyu adzati, *“ndipempherere ine! Umufunse Yesu adzandithandize! Chonde Iwe ndithandize ine? Ndikuyitanira iwe kulankhula mau ndi nzeru za Yesu kwa ine nthawi zonse. Ndidzatsegula mtima wanga ndipo ndidzalandira kuwala ndi choonadi ndi Unsembe wake wa okhulupilira onse.”*

Kodi munthu wampando wachiwiri anganene chiyani? Munthu uyu alibe Mzimu Oyera. Munthu uyu akhonza kuwoneka kuchita zozizwa mu dzina la Yesu. Munthu akhonza kuyimba ndi kuvina ndipo ngakhale kulalika, komabe alibe Mzimu Oyera. Kodi mukudziwa kuti munthu uyu alibe ndipo ndiosapulumsidwa kwenikweni? Chifukwa pamene mupita kwa munthu uyu ndi kunena, *“khalidwe lako silabwino m’mene uchitira mkazi wako,”* munthu uyu amanena, *“kodi ukundiweruza ine! Chotsa chipika chakocho pamaso anga! Ukhala walamulo iwe! Samala za machitidwe ako! Kodi ukuwona ngati ndiwe ndani ukandiyankhule ine choncho? Usakhudze ozozedwa wa Mulungu!”* Munthu uyu siopulumutsidwa chifukwa munthu uyu sakonda kuwala. Pali umboni wa mphamvu kuti munthu uyu alibe Mzimu Oyera, chifukwa munthu uyu sakonda kuwala. Ena anakonda kuwala ndipo tsono ali opulumutsidwa. Ena anadana ndi kuwala ndipo ali osapulumsidwa (2 Atesa. 2:10). Ena anakonda kuunika ndipo ena anadana ndi kuunika chifukwa cha zochita zawo ndi zoipa (Yohane 3:19-21).

Tsono ngati muweruza kudzera m’makhaliidwe, mudzasokoneza. Nthawi zina khalidwe la anthu ampando wachiwiri ndi wachitatu limaoneka lofanana. Mu zoono, nthawi zina ampando wachiwiri, amaoneka pa nthawi, kuti akupanga zinchito zabwino m’malo mwa Yesu. Koma Yesu mu Yohane 3, ndi Mtumwi Yohane mukukalata wa Yohane Oyamba anena khalidwe silimene munthu wungaweruzire. Inu mukhonza kumvetsetsa za amene ali ndi Mzimu. Ndipo chifunguro cha umboni chakuti Mzimu wukukhala mkati mwa munthu ndi m’mene munthuyo apangira ku kuwala.

Pangano latsopano

Ndidzapitanso kumbuyo mu Chipangano Chakale kuti ndionetsere mfundo iyi. Uneneri okhudzana ndi kubwera kwa Yesu ku Chipangano

Chatsopano ukhonza kupezeka mu Yeremiya 31 ndiponso mu Ezekiele 36. Mumalo onse awa, Iye adanena chinthu chimodzi chokhudzana kubwera kwa Pangano Latsopano. Mulungu adati kuti Mupangano Lakale munthu amanena kwa mzake, “Mudziweni Ambuye!” (Ife tayetsetsa kubwezeretsa Pangano Lakalemu mpingo mfundo yolakwika).

Pangano Latsopano, kutengera kwa onse Yeremiya ndi Ezekiyele, ntchito ngati izi: “Umboni oti ndakhulukira machimo awo ndipo sindikukumbukanso zoyipanso zawo, umboni oti ndakhulukiradi machimo awo ndipo ndawapanga iwo akhristu oti ndidzayika Mzimu wanga mwa iwo ndipo ndidzapanga iwo kusungalamulo langa.” Umboni oti munthu ndi mkhristu weniweni ndipo machimo awo ndi okhulukidwa, kutengera ndi uneneri wa zaka mazana asanu ndi limodzi pasanafike nthawi ya Yesu, ndilo kuti Yesu adzayika Mzimu wake mwa iwo ndipo Iye adzatembenusa mitima yawo yamiyala ndi kukhala mitima ya mnofu. Iye adzayika Mzimu mwa iwo ndi tsopano nkhoa zidzadziwa mau a m’busa.

Umboni wa mzimu oyera

Mkhristu, olengapo gawo la pangano latsopano, amakonda choonadi (2 Atesa. 2:10) ndipo amakonda kuunika (Yohane 3:19-21) ndipo tsopano ali “otengapo gawo la chilengedwe CHAUZIMU” (2 Petro 1:4, Aroma 6:1-14). Uwu ndiye umboni woti Mzimu umakhala mwa iwo kapena mwa wina aliyense wa ife. Ife sitiyenera mau a aliyense pakuti chifukwa akuti, “Ambuye, Ambuye! “Iyi ndi nkhani yabwino! Amafano kapena azipembedzo zonyenga sangalamulirenso Mipingo! Ife tikhonza kumvera tsopano, kuchokera mu ubale, ulamuliro oti “chotsani chotupitsa mu mkate” wapanda kukhala “moweruza!” Ngati iwo samakonda kuunika kwa kuonetsera chifukwa amakhumbitsitsa kukula mwa Yesu, koma koposa amathawa ndi kukana kutsekereza ena kudzera mkudzitchinjiriza, siali opulumutsidwa, kutengera kwa Yesu, ndipo sangatengedwe kukhala gawo la Mpingo Wake. Tsopano, kumbukirani: NDI CHIBALE CHATSIKU NDI TSIKU CHOKHA chimene mungadziwire ngati aliyense akonda kuwala ndi choonadi ndipo potere ali mwana wa Mulungu. Misonakhano yochepa pasabata sidzalola aliyense kudziwa ngati wina wake amakonda kuunika ndipo ali chabe ofooka, kapena ngati iwo amadana ndi kuunika ndipo potero siali opulumutsidwa. Ngati iwo sakonda choonadi ndi

kukhumbira icho ndi mitima yawo yonse (koposa kukana mchoonadi ndi kunyada ndi kudziteteza ndi kutsatsirana kulakwa). Kenako Mzimu Oyera amanena kuti iwo siopulumutsidwa konse. Ichi ndicho chothandiza kwambiri kumvetsetsa: Ngati iwo ali opulumutsidwa, ADZAKHALA ndi Mzimu Oyera (Aroma 8:9, Agalatiya 3, Aefeso 1). Ndipo UMBONI oti iwo ali ndi Mzimu Oyera mwa iwo (ngakhale nthawi yambiri bwanji iwo akuuzani iwo “umboni” waukulu ndipo anena, “Ambuye, Ambuye! “Mateyu 7) ndi oti amakonda kumvera. Ali obadwa atsopano ndipo amakonda kuwala ndi kukonda choonadi, (2 Thess 2:10) ndipo monga makanda amakonda mkaka ndi mau a Mulungu kuchitidwa mu moyo wawo (1 Petro2).

Mu Chipangano Chatsopano sitikakamiza munthu kudziwa Mulungu. Sitinena kuti “sintha makhalidwe ako kuti ukhale Mkhristu tsopano tinganene”. “Khalidwe lako silili ngati la Yesu”. Okhulupilira wowona monga makanda akonda mkaka amati, “zoona” Mulungu andikhulukire ine mungandikhulukirenso ine 1 Akorinto 12 ndi Aefeso 4 amati ndili kufuna kuthandizidwa kuti ndikhale monga wa Yesu. Mungandithandize chonde mundipempherere ine ndipo ngati mungawonenso ndili kuchita chomwecho chonde bwerani kwa ine ndipo ngati sindili kumveranso inu bwino, chonde tengani awirii kapena atatu bwerani ndi kulankhula ndi ine mu njira imene Ambuye ndi okondedwa Yesu anatilamulira.

Mukumbukira malembo mu Mateyu 18? Ngati mulankhula kwa mbale kapena mlongo ndipo poyamba sakumva ndi kudziwa bwino, Yesu amati tengani awiri kapena atatu kuti athandize kuti amvere. Ndiyenso ngati samveranso ndikuti sakusinthayankhulani ndi mpingo wonse. Sizimene Ambuye athu anatiphunzitsa?

Onani pa mtima, osati makhalidwe

Mtima ndi choonera kuti Mzimu Woyera uli kukhalamkati mwa munthu. Mphatso ya Mzimu Woyera uli kukhala ndi dipo limene limatipatsa cholowa chathu, ichi ndi chiweruziro chake amatero Yesu mu Yohane 3. Ichi ndi chimene chimatisiyanitsa osalakwa ku chiweruzo. Osati aliyense ndi wabwino, koma amene machimo awo akhulukidwa onse ndi kukonda “kuwunika”. Ali ndi mphatso ya Mzimu imene sanali nayo

poyamba. Tsopano kuchokera pansi pa mitima yawo yowuma tsopano ndiwofewa. Pansi pa mtima Mulungu ali kuwalamulira kusunga malamulo ake. Kuchokera pansi pa mtima amasamala Yesu mau ake pa makhalidwe awo. Pansi pa mtima mau a mbusa amadziwa chifukwa ali ndi Mzimu wa Yesu nkhusa imati! ndili kufuna Yesu nditsogolereni” Mbuzi zimati ndisiyeni ndekha! Ndimachita zozizwa! Ndingapereke chuma changa kwa aumphawi. Ndimadziwa zinthu. Ndiri wabwino koposa iwe ndipo sindisamala pa zokamba zanu”.

Kuwonera pa makhalidwe sinjira yabwino ku dziwa mtima ngati khalidwe la munthu ndi loipa ndi chidziwitso choti pali bvuto. Koma ngati simungalankhule kwa iwo chifukwa sakonda kuwala ndiye kuti muli ndi bvuto lalikulu. Munthuyo ndi osapulumsidwa ngati kumbali ina munthu ndi kutheka kuti ali choncho chifukwa choti ali khanda chabe ndipo khalidwe lokhalo ndi bvuto.

Sakudziwa za izi bwino, koma amakonda kuunika ndipo ali kufuna kuthandizidwa izi ndi zotheka kukoneka.

Tisangoona pa bvuto la khalidwe lokha . anthu ambiri ali ndi mabvuto, chifukwa mwina makolo sanawalere bwino. Enanso mwina anali ndi abwenzi amene anali ndi magulu asanakhala otsatira AYesu. Mwina asanabwere kwa Yesu anali mu uchimo waukulu (mmene ndinali ndi inu nomwe) ndiye tinabwera mu ufumu ndi mukhalidwe ambiri oipa) ndibwelezenso, nkhani kodi timakonda kuunika.

Mukumbukila chitsanzo cha malemba? Okhulupilira aku Akorinto anali akhristu oyamba kumene. Palibe amenen anali a khristu kwa zaka zoposa zitatatu kapena zinayi. Anali kukhala mu mzinda yoipitsitsa otchedwa Akorintho unali ndi zoipa, monga kugonana okha-okha amuna ndi zinthu zina zambiri kulingana ndi kalata ya Paul okhupilira amenewa anali atachoka muzoipa zoipitsitsa komabe anali makandabe. Anali atapeleka miyoyo yawo kwa Yesu. Koma anali ndi zofooka ndi makhalidwe oipa choncho makhalidwe awo sanali abwino koma mukudziwa zimene Paulo ananena pamene anakomana ndi mabvuto amenewa? Anati, ndimadziwa kuti mudzamvera.

Mukalata ya chiwiri kwa Akorintho, mu mutu 7 Paulo anati, pamene mudalandira kalata yanga yoyamba munayankha ndi mphamvu ndi kulapa

kwakukulu. Munaopsedwe ndi uchimo umene unalipo mu miyoyo yawo. Munakhudzidwa ndi uchoyo ndipo mudakonzekera kuuchotsa Paulo anati ndinamuuza Taitasi kuti timadziwa

Kuti pamene mulandila kalata yanga kuti mudzalapa ndi zimene Akorinto 2:7 amanena.

Makhalidwe awo anali oipa mu mpingo wa Akorintho Paulo analemba kalata yoyamba kwa iwo ndikuthandiza za uchimo wosiyanasiyana. Koma ndithu anali woomboledwa ndipo Paulo amadziwa kuti anali opulumutsidwa ndiye anali oyera choncho ndimadziwa kuti mudzalapa ndipo ndinamuuza Taitasi kuti walapa. Choncho tsopano Taitasi wabwera kwa ine ndi kundibweretsa uthenga wachikondi ndipo chabweretsa chimwemwe mu mtima mwanga kuti mwalapa monga mmene ndinamuuza. Aliyense amene ali ndi mzimu woyera amalandira kalata yochokera kwa mbale yomuthandiza. Amamfuna kuthandizidwa.

Uthenga wabwino ndi woti Yesu Khristu ndi oti tinatchulidwa ndi mwazi ndi kuti machimo athu onse anakhululukidwa chifukwa tinaika chikhulupiliro chatu chonse mwa Yesu monga mpulumutsi. Chitsimikizo choti tachita zimenezi kuchokera mu mtima, ndipo omwe amasindikiza za cholowa zathu, ndikuti mzimu woyera waperekedwa kwa aliyense amene ali woona mtima ngati munthu ali ndi mzimu oyera adzakonda kuwala ndi kukonda chowonadi... Ndiye kenaka khalidwe lawo lidzasintha. Amalapa pa zimene alikuchitira ndi amuna awo kapena akazi awo ndi kusintha. Amalapa mmene amakhalira ndi ogwira nawo ntchito, kapena ana awo kapenanso ozungulira nyumba zawo ndipo makhalidwense oipa ndi kusintha ndi kukhala akulu msinkhu.

Chikonzero cha Mulungu kuti ife tikule tsopano

Mukuwona m'mene mpingo umakhudzidwira ndi nkhanayi? Chikonzero ndi chuma chobiisika pansi pa nthaka. Chikonzero cha Mulungu ndi choti unsembe ya okhulupilira. Pulani ya Mulungu ndi kwa anthu ake ndi kumangilirana wina ndi mzake tsiku ndi tsiku monga timakhalira moona ndi tonse pamodzi choyamba chopindulitsa ndi chakuti onse amene ali ana a Mulungu amakula ndi makhalidwe abwino. Zabwinonso zimene zimakhala poyenda pamodzi ndi Mulungu ndi choti, ngati wina

sakonda kuwala, amawonekera kuti ndi onama chabe. Ngati ndi wosafuna kukonzeka, ngati sasamala pazimene Yesu ananena pa zinthu izi ngati amakwiya ndi kupsya mtima pamemepo amaonetseredwa ngati a khristu onyenga. Zimawonekera kuti sanapeleke moyo wawo kwa Yesu chifukwa alibe choonadi ndiye satha sangakhale ndi Mzimu Woyera ndiye kukhala osakonda kuwala (Yohane 3, 1 Yohane 1, 3).

Choncho ngati mpingo ndi mpingo woona, ndiye ngati ansembe tonse tidzathandiza kuti tikhale ndimakhalidwe abwino. Tidzakhala tonse kuwala ndi moyo wina ndi mzake. Tidzathandizana wina ndi mzake kuwona zinthu zimene sitingathe kuona tokha. Ngati ndili wodzikonda, sindingathe kuona kudzikonda kwanga. Kudzikonda kwanga kuli kuwawitsa Yesu. Kudzikonda kwanga kuli kuononga kuthekera kwanga kukonda Yesu. Ngati ndili ndi kudzikonda zili kuwononga kudalitsika kwanga kwa Mulungu chifukwa Mulungu safuna kudalitsa kuzikonda kwanga. Zimawononganso umboni wanga wa Yesu ngati ndili wozikonda motero cholinga cha unsembe ndikuthandizana kudziwa Mulungu bwino tsiku ndi tsiku. Mu msika, ku nyumba zathu pamalo athu mu mpingo. Ndingakule kuchoka mu mkanda la kuzikonda ndi kukhala munthu wa Mulungu.

Paulo anati, 1 Akorintho 3) kuti anthu ambiri amene anapulumuka amakhala atachoka mu lawi la moto. Anthu awa amapita kumwamba koma atadutsa mu Malawi a moto pofika kumeneko. Werengani 1 Akorintho 3 nokha. Baibulo limati anthu ena anapulumutsidwa koma atadutsa mu malawi a moto koma ichi sicholinga cha Mulungu. Sizimene Mulungu amafuna kuti ife tikalowe kumwamba. Cholinga cha Mulungu ndikuti osati kuti tikhale makanda ndi uchimo kenaka ndi kupita kumwamba. Cholinga cha Mulungu ndikuti ndife mudzi oikidwa pa mwamba pa phiri umene sungabisidwe cholinga cha Mulungu tikhale oikidwa monga mfumu pa mapiri. cholinga cha mulungu ndi choti kuti mkwatibwi amene wakonzekera kale. Cholinga cha Mulungu ndi choti ndife wowengeka, omanga banja ndi mkwatibwi omanga uchimo. Cholinga cha Mulungu ndikuti mpingo ukhale okonzeka mwana wa Mulungu pamene abweranso kwa mkwatibwi.

Aliyense ndi wololedwa kwa Mulungu kukhalamu mpingo amene akonda kuwala. Ena aife tikhonza kukhala aang'ono. Ena a ife tingakhale ndi

khalidwe loipa kwa nthawi zina koma ngati tili ndi mzimu wa Mulungu ngati tili ndi akhristu osati akhristu onyenga – ndiye kuti tili kukonda kuwala. kukonda kuwala pamodzi ndi abale ndi alongo. Tidzakwanitsa kuthandizana wina ndi mzake kukula. Ndiye kuti aliyense adzakula ndi mphamvu ndi mphamvu ndi nzeru . Tingakhale okonda Yesu ndi mphamvu zambiri ndi moyo wathu. Umboni wa Yesu ukhonza kukhala wa mphamvu koposa ndi kuononga mdaniwo sipazakhala ana okha okha ndi makhalidwe oipa amene angaoneke osati ngati Yesu.

Ana ambiri ang'ono ndi a makhalidwe oipa sizakondweletsa kwa makomo a ndende. Ana ambiri ang'ono ndi amakhalidwe oipa sizodzathandiza osakhulupilira kuti atsate Yesu.

Ngati tili mpingo wa amuna ndi akazi a Mulungu amene ali okhwima ndi kumaoneka ngati Yesu ndi moyo wathu ngati mpingo ndi wopambana, nzeru, mkwatibwi wopambana wa Yesu ndi mphamvu ya Mulungu ndi khalidwe la Mulungu mu moyo wathu ndiye anthu adzakhala okondwa ndi Yesu ndipo adzafuna kubwera kuti adziwe Yesu.

Choncho lingalirani za Chikhristu chonyenga mpando wa chiwiri) ndi kuti Mkhristu weniweni (mpando wachitatu, wachinayi ndi wachisanu) Lingalirani kuti khalidwe loipa sizotikuti ndiye sanasambitsidwe ndi mwazi wa Yesu. Nkhani yeni yeni monga mu Yobu 3, Yohane 1, 2 Atesalonika 2 ndi Petro 2 ndi yoti Mkhristu woona ali ndi Mzimu wa Mulungu. Inde makhalidwe ake angakhale oipa monga mwana pa makhalidwe ake sakhala abwino koma ngati anabadwa kachiwiri ndi Mzimu ndipo monga makanda adzakhala akumwa mkaka adzakula mu choonandi ndi kuunika. Cholinga cha mpingo ndi kuthandiza munthu ameneyo wa makhalidwe oipa amene amakonda chowonadi kuti akhale ndi nzeru ndi kulimbika mtima poopa Yesu ndi kukula msinkhu.

Choncho tiyenera kumasulira Mkhristu motere ndiponso tiyenera kukhala monga mpingo uyenera kukhalira. Kuthandizana wina ndi mzake tsiku ndi tsiku kuti wina asaumitsidwe kapena kunamizidwa ndi uchimo. Tiyenera kukhala ngati ansembe. Ndipo ana ang'ono adzakula ndi mphamvu.

Yesu adzakhala ndi umboni:- Mkwatibwi adzazidwa ndi Mzimu ndi mawonekedwe ake. Yesu adzakhala ndi mpingo umene makomo andende sadzatha kugonjetsa. Motero kukongola kwa Yesu kudzakhala kwa Isilamu

onse ndi kuchita uHindu kuti onse awona kuno konse. Tisakhale makanda chabe amene amanena bwino zinthu. Koma osakhala monga Yesu ndipo Mpingo sikupeza anthu onyengezera chabe amene amakhala bwino chabe koma alibe Mzimu wa Yesu okhala mwa iwo monga munthu. Koma tikhonza kukhala opambana namwali wa Yesu uwu ndi uthenga wa bwino wa ufumu wa Mulungu.

Mphamvu chosintha, mphamvu yowonetsera

Tsopano tibwererense ku machitidwe a mipando isanu ija, Anthu amene angakhale mu mipando wa chiwiri, wachitatu, wachinayi ndi wachisanu ali opezeka ku Bapatisiti, Nazarene, Methodis ndi ma Pentekositi mu misonkhano awo. Chifukwa tamanga molakwika mpingo ndipo anthu onsewa ali pamodzi. Mipando isanu yafanizira ija. Kuphatikizira ndi mpando wa chiwiri umene suloledwa mu mpingo ngati mamembala koma posowa chilungamo, chiyanjano mu tsiku ndi tsiku mu unsembe (monga Mulungu amafanizira ndi kulumulira) wa pa mpando wachiwiri amaloledwa (mukusamvera kwa Ambuye) 1 Akorinto 5). Monga ali oipa ndipo wa mu mpando wachitatu nthawi zone amakandira kapena osafunidwa, zoona zake ndi zoti 85% ambiri amene amaloledwa mu mpingo kuli konse ndi mpando wachiwiri kapena wachitatu. Uku ndi zomvetsa chisoni ndi zosafunikanso ngati tili kumanga mu njira ya Yesu. Posakhalitsa tidzakhala ndi Chisilamu kapena mu Hindu amene tidziganiza kuti ali chiwalo cha mpingo.

Koma chimbedzo kungokhala mwa mpingo wa chipembedzo (siumene mpingo umene mulungu amafuna kuthandinzira) umene uli ndi onse inali ya anthu pamodzi. Mukuvetsa zimenezi?

Ngati tikhala mnjira imene Yesu ananena ndi kuyamba kumanga njira imene mpingo uyenera kumangidwira, ndiye tikhonza kudziwa amene ali ongonama chabe kapena amene ali opanda mphamvu ndipo tingawathandize. Ngati mpingo ungamangidwe pozungulira mu mgwirizano mmalo mwa msonkhano wa lamulungu ndiye onse anthu amitundu inayi idzakhala ndi kulumikizidwa tsiku ndi tsiku. Onama ndi ana enieni. Atate ndi anyamata adzakhala mu mgwirizano ndi wina ndi mzake Kukonda wina, kuthandizana ndi wina zobvuta kukwaniritsa

lamulo la khristu. Ngati mmenemu ndi mmene mpingo ungaonekere, ndiye muli ndi mphamvu zosintha zinthu ndi kuzionetsa poyera.

Mukukumbukira mu Machitidwe 2:42-47 kuchokera tsiku loyamba chikhristu onse ali pamodzi okhulupira ndipo anali ndi zofanana? Izi sizinali chifukwa cha “chikhalidwe” kapena zochita – zidali anthu okhala mu moyo ndi chipulumutso cha Yesu. Anthu lero amakhala kumbuyo kwa zokangana za chikhalidwe kuonetsera kuti amakonda dziko ndi zinthu za mziko ndi kufuna mulungu wa la mulungu mmawa ndi lachitatu usiku ndi magulu okumana lachisanu. Koma anthu a mulungu obadwa kuchokera ku mwamba ndi Yesu, poyamba ndi zofunika tsiku ndi tsiku ndikukhala onse pamodzi nyumba ndi nyumba. Anali onse tsiku ndi tsiku kukhala mu chiphunzitso cha Atumwi, kukhala mu chiyanjano kunyema mkate, kupemphera. Sanali ongofanana mu zinthu zina Mach 5.4.5 koma moyo watsopano kuchokera mwa iwo monga Yesu analamulira kuti zinthu zonse sizinali zawo zawo. Baibulo limati anali anthu alukana pamodzi monga mithempha ukhalira. Uwu ndiwo mpingo wa chipangano chatsopano-Tsiku lililonse. Mgwirizano wawo, aliyense wa iwo anali ndi amayi ambiri, abale, ndi alongo ngati ndi m'mene tingamangire pali mphamvu ya mulungu wosintha mphamvu yoonetsedwa ndi kuchotsa malinga a satana mu moyo wathu.

Tiyenera kumanga mu njira ya mulungu

Ngati tikumanga mu njira imene anthu anamangira ndi miyambo ya anthu pokhala ndi mmawa wa la Mulungu ndi ulaliki ndiye anthu awa amene ali mu mpando wa chiwiri umene amangosoneyeza anthu odzangowonerera chabe tsopano 1 Akorinto 5 limanena kuchotsa chotuopitsa. Baibolo limanena kuti ngati pali ojedana pakati panu, achiwerewere, odzikonda, opembedza mafano kapena anthu amene amakonda dziko lapansi tiyenera kuwachotsa mu msonkhano. Mau a Mulungu amati ngakhale osadya nawo pamodzi amene amati ndi .okhulupilira koma osakhala nawo mu njira ya Mulungu. Tisakhale nawo pamodzi kapenanso kukhala abwenzi athu. Yesu anati tiyenera kuwathamangitsa. Baibolo limati aliyense amane amati ndi mbale koma amakhala mu uchimo ayenera kuchotsedwa pakati pa msonkhano. Tsopano, mungachite bwanji zimenezi ngati ndi lamulungu mmawa. Kapena ndi moyo wokha womwe ndi wowonekera mmawa okha.

Chifukwa chiyani sikothekha kumvera malemba amene amanena kuti tikhale amodzi ndi kuchotsa chotupitsa? Chifukwa tamanga molakwika. Chifukwa mmene tamangira ndi miambo ya anthu, munthu uyu wofooka (wa mpando wa chitatu) amaoneka oipa. Ndi munthu winayo amene sanapulumsidwe wa pa mpando (wachiwiri) amawoneka ngati ndi opambana nthawi zambiri. Nthawi zina ndi Dikoni kapena mkulu wa mpingo, kapena ndi mbusa ndipo wa mpando wa chiwiri amachita zozizwa mu dzina la Yesu la Mulungu mmawa munthu uyu ndi otsuka koma salinso mkhristu ndipo munthu wa pa mpando wa chitatu ndi ofooka. Koma munthuyu ndi opulumutsidwa ndipo munthu uyu wa chiwiri amene sachita mau ndipo sakonda kuwala. Munthu ameneyu sali opulumutsidwa ayi. Ali chotupitsa, ndipo Mulungu salikulola kuti akhale pamenepo.

Anthu ena amagwiritsa chiphunzitso cha Yesu mu mwambi wa Tirigu ndi na Msongole (Mat 13) kulola uchimo wa Mpingo, pomati tiyenera tiyenera kulola tirigu ndi na msongole kukulira pamodzi monga Yesu ananenera. Angelo ndiwo adzamalize nchito yonse ku mapeto anthawi yino. Uku ndi kulakwa kwakukuru ndikusiyanyitsa ndi chimene Yesu ananena nthawi zina mmodziwa kapena mosadziwa pa zofuna zawo). Werengani Fanizo limeneli pa inu nokha, ndipo mudzaona kuti Yesu Sali kuchotsa chimene Paulo, mwa mzimu analamulidwa kuchotsa chotupitsa pakati abale Yesu sanati, “Muyenera kusunga udzu pakati pa mpingo- Yesu anati Munda ndi dziko, Yesu sanati mundawo ndi mpingo, zoono tili mu dziko lapansi koma osati mu dzikomo ai nkidipo mdani adzabyala udzu mdziko la pansi. Sitikufuna kuti tingobweretsa zinthu zina zake zosamveka ai mudziko pakuchotsa udzu kuchoka ku dziko. Ife tiyenera kukhala mchere ku dziko lapansi ndi kuunika kwa dziko lapansi ndi zimenezi anthu onse azdadziwa kuti muli ophunzira anga”! Mpingo wuyenera kukhala pamwamba pa phiri ndipo sungabisike, choncho kuti awone machitidwe anu ndi kutamanda Mulungu pa tsiku limene lilinkudza. Tiyenera kulola udzu kukula pakati pa tirigu MU DZIKO LAPANSI” Mwachoncho Yesu sanati, Munda ndi Mpingo. Udzu ndi tirigu sukulira pamodzi mu mpingo monga mwa Mulungu.

“Kudzitamanda kwanu sikuli bwino. Kodi simudziwa kuti chotupitsa pang’ono chitupitsa mtanda wonse? Tsukani chotupitsa chakale kuti mukhale mtanda

wa tsopano monga muli osatupa. Pakutinso Paskha cha Dumbo, kuipa mtima, koma ndi mkate osatupa wakuona mtima, ndi choonadi.

Ndinalembera inu kalata uja kuti musayanjane ndi achigololo, sikonse konse ndi achigololo adziko lino la pansi, kapena ndi osilira ndi okwatula kapena ndi opembedza mafano pakuti mukutulule mdziko lapansi. Koma tsopano ndalembera inu kuti sayanjane naye ngati wina wochedwa mbale ali wa chigololo, kapena wosilira kapena wopembedza mafano, kapena olalata kapena oledzera, kapena olanda, kungakhangale kudya naye otere iai.

Pakuti nditani nawo akunja kukaweluzwa iwo? Kodi amene ali mkatimu simuwaweluzwa ndi inu koma akunja awaweluzwa Mulungu? Chotsani oipayo pakati pa inu nokha (1 Akorinto 5:6-13).

Yesu sanazidzutsa yekha inde munda umene Tirigu ndi Namsongole umakulira pamodzi mpa nthawi ya kutha kwa dziko lino. Si mpingo ai, monga mwa Yesu, “Munda ndi Dziko” musalore ena kudokoneza inu uthenga wa kusamvera ndi onyengelerwa.

Tsopano muziwoneka bwini, ngati tingayembe kumanga bwino, mu njira imene Baibolo limanena kuti mpingo uyenera kumangidwira, ndiye kuti onse anayi anthu adzakhala ndi maubwenzi abwino tsiki ndi tsiku munthu uyu wachiwiri amaoneka mngati otchuka mu msonkhano amayimba bwino ndipo amadziwa Baibolo kwambiiri siwabwino ameneyo! Koma ngati muli ndi mgwilizano wa tsiku ndi tsiku mungawone kuti amadana ndi mkazi wake. Mukapita ku nyumba yhake la chiwiri mungawone kujti ali kukalipira ana ake ndipo mukapita lachinayi madzulo kukawelenga malembo ndi iye mukapeza kulibe kuti kunyumba kulibeko. Mukafunsa mkazi wake “Ali kuti amuna anu” Ndikufuna kuwelenga naye pamodzi malembo ndipo amati, “sitikudziwa kumene apita” salinso ku offesi angochoka, amabwera mochedwa ndipo sanena kuti, ali kuti” Mungadziwe zimenezi la mulungu lokha mmawa mungawone kuti munthuyo amakonda dziko ndipo ali ndi moyo wanseri ngati Sali kunyumba yake yachinayi usiku. Sadzavala chizindikiro cholembedwa Ine ndine wonyanga ndipo ndili ndi moyo wa chinsinsi, ndiye munganene kwa iye ndinabwera ku nyumba kwanu kudzapemphera nkdi inu kudzawenga malembo dzulo madzulo ndiye inu kunalibe kumeneko. Munali kuti? Akazi anu samadziwa kumene mwapita? Munali ndi abale ena kukagawa moyo wa Yesu mu msewu?

Amayankha, “Ai sichoncho. Sizikukukhudzani ai. Ndipo mukati chabwino chifukwa chiyani mukutero? Ndingadziwe chifukwa chache. Sizikukukhudzani ai. Chotsani chisoso chanu mmaso anu. Bwanji muli oweluzi ine motero ndimalamulo. Chabwino, ndamva kumene mukuchokera ndipo ndikukupemphani kuti mufewetse mitima! Mwinadi palibe chobvuta koma timangofuna kufunsa, chifukwa ndikukhuzidwa ndi mtima wanga koma simungalire kuti tilankhulanabe kuti ndidziwe? Ai samalani zanu.

Chabwino choncho ndiyenera kuchita zimene Yesu ananena kuti tizichita mu zinthu ngati izi ndipo tiganize kuyitana abale ena kuti tipitilize kulankhulana pa nkhani imeneyi aliyense amene mungaganiza amene tonse tinagulitsidwa kwa Yesu ndipo ndiwozindikira zinthu? Yesu anandilamula ine kutenga enga awiri kapena atatu ena kuti tilankhule za zinthu izi chifukwa choti ndiotsatira ake a Yesu muyenera ,kumvera Yesu pobweretsa ena awiri kapena atatu ndipo tikhale pansi ndikulankhulana za izi, akanena kuti sindifuna kuti ndilankhulane ndi ena abale awiri kapena atatu ndikuti musamale zanu osati za ine

Ndiye mumadziwa kuti ooh tili ndi mavuto akulu pano ngati sizisinha, ndiye kuti safuna kukonda kuwala kapena kukonda chowonadi, ndichitsimikizo choti ndichotupitsa chimene ndichofunika kuchoka pa mpingo ngati palibe kulapa.

Tsopano tingadziwe bwanji kuti tili ndi zobvuta m’banja? Munthu uyu anali wa mphamvu pa la mulungu mmawa ndingadziwe bwanji za munthu onyenga amene ali ndi miyoyo yiwiri? Tikadziwe ngati tingapite kwawo la chinayi madzulo. Pomaliza, timadziwa kuti mbale uyu sanali kukonda kuwala chifukwa sanali kukonda kuwala ndi mboni yoti analibe mzimu wa Yesu. Safuna kusinha, sasamalira pamaganizo athu. 1 Akorinto 5 limati ngati wina azitcha yekha mbale koma kukhala mu uchimo osadya naye, osakhala naye pamodzi ngati bwenzi ndipo achotsedwe pakati pa abale. Ngati tingamange mmene anthu amangira ndipo sitidzadziwa kuti pali vuto ndi munthu mumoyo wake ndiye chikumbumtima chake ndichoumitsidwa. Koma ngati tingamange mnjira imene Yesu ananena kuti timange potengerana zothobwitsa, wina ndi mzake tsiku ndi tsiku mwina munthu uyu adzakhala munthu wodlalilika.

Wonani abale kuti kapena ukhale mwa wina wa inu mtima wiopa osakhulupilira, wakulekana ndi Mulungu wa moyo komatu dandauliranani nokha tsiku ndi tsiku pamene pachedwa lero kuti angaumitsidwe wina wa inu ndi chenjero la uchimo. Pakuti takhala wolandirana ndi khristu ngatitu tigwiritsa chiyambi chakutama kwathu kuchigwira kufikira chitsiriziro. (Aheberi 3:12-14).

Ngati tingamange mu miambo ya anthu ndi kulalikira kwa lamulungu ndingaganize kuti munthu uyu ndi mkhristu koma Mulungu akuti “Sindimudziwa iye” Tingamuthandize bwanji ku uchimo ndi kuwukira kapenanso kukonda dziko ngati sanawonekere?

Nthawi zina kulalikira kumachitika pakati pa miambo ya anthu kwa anthu amene amaganiza kuti ndi akhristu?

Ngati mungamange mnjira yabwino tsiku nkdi tsiku kuchokera mu zinyumbandizinyumbandiye kuti uchimo udzawonekera ndipo tidzawona ngati ena li kukonda kuwunika ngati sakonda kuwunika ndiye timawayika kumene ayenera kukhala monga mmene Mulungu amanenera, “Achotseni pakati pa abale ndipo munthu uyu sakhalanso otchukanso ayi adzayamba kuganiza za moyo wake chifukwa sakhalanso monga mmene analiri kale ai mwaina tsopano ndi mmene angakhale mkhristu weni-weni.

Kapenanso mukumanga munjira ya Mulungu tinapeza chuma chimene siitinachidziwe ngati tili monga mmene Mulungu analamulira kukhudzidwa ndi miyoyo ya mabanja ndi zodabwitsa zizawoneka zimene siziwoneka ku magule ena kapena lamulungu mmawa. Ngati tidzakhala monga Mulungu afunira wokhala tonse ndi chikhulupiliro chimodzi tonse ngati munthu mmodzi ndipo wokhlupilira onse anali pamodzi ndipo zodabwitsa zidzakhalsano. Koma kufuna ufumu osati kukhala wodzidalira tokha kuchotsa miyoyo yathu kuchokera muthupi ndi mwazi koma mukubadwando mu mzimu.

Mbiri ya dziko yasonyeza kuti anthu amene mu mpando wa chiwiri ndamene ali atsogoleri koma ndiosapulumsidwa! Kodi munamva za munthu wotchedwa Charles Finney? Monga munthu wa mkulu anali mtgsogoleri wa woyimba koma adazindikira kuti sadali mkhristu ndipo anabadwanso ndikukhala munthu wa Mulungu. Charles Finney anabweretsa anthu 500 000 kwa Yesu mu nthawi ya moyo wake mukudziwa

kuti iye anali wodzikpereka ndi wachipembedzo mukukula kwake koma anadziwa kuti sanali mkhristu ai ndipo anasinthika mu mtima ndikukhala munthu wa Mulungu ndingatchule ambiri ena amene timawadziwa kuti ndi anthu amphamvu a Mulungu kuchokera mu mbiri anali atsogoleri mu chikhristu koma anazindikira kuti sanali akhristu ai.

Mbiri ya dziko yasonyeza kuti anthu amene mu mpando wa chiwiri ndamene ali atsogoleri koma ndiosapulumsidwa! Kodi munamva za munthu wotchedwa Charles Finney? Monga munthu wa mkulu anali mtogsogoleri wa woyimba koma adazindikira kuti sadali mkhristu ndipo anabadwanso ndikukhala munthu wa Mulungu. Charles Finney anabweretsa anthu 500 000 kwa Yesu mu nthawi ya moyo wake mukudziwa kuti iye anali wodzikpereka ndi wachipembedzo mukukula kwake koma anadziwa kuti sanali mkhristu ai ndipo anasinthika mu mtima ndikukhala munthu wa Mulungu ndingatchule ambiri ena amene timawadziwa kuti ndi anthu amphamvu a Mulungu kuchokera mu mbiri anali atsogoleri mu chikhristu koma anazindikira kuti sanali akhristu ai.

Choncho chinthu chabwino chimene tingachite ndi munthu amene sakonda kuwala ndi kumvera zimene Yesu ananena ndi zimene Paulo ananena “pitani kwa iwo okha” ndikuyesa kuwapindula ngati apitilira mu uchimo ndipo safuna kumva ndiye tengani awiri kapena atatu ena ngati sakonda kuwunika ndi kusasamala ndiye tiyenera kumvera Mulungu ndikuwachotsa iwo mu mpingo mwina moyo wawo wungapulumsidwe chifukwa tagwiritsa chida chimene Mulungu anatipatsa ife kuti achenjezedwe. Sitichita izi mu mkwiyo ,kapena mu kuziyenereza tokha oyera. TimachitaIzi mu kumvera Mulungu .

Timakonda iwo. Timafuna kuti asinthike mtima moona ndithu Osati kunyengedwa chabekwa mtima. Ichi ndi chida chimene mulungu wapereka kwa ife potandiza anthu kuti azindikire amene ali mu chipembezo koma onamizidwa.

Mpaka titathandizana wina ndi mzake tsiku lililonse ndi kukhala ndi mgwirizano weni weni tsiku ndi tsiku munthu mu zochita zake zenizeni sizingatheke kudziwika baibulo limati chotupitsa pang’ono chimatupitsa mtanda wonse, choncho ngati munthu ali ndi chinsinsi cha

uchimo mu umoyo wake ndipo sanathane nazo ndiye kuti anthu onse a mulungu amapwetekeka chifukwa cha chimenechi. Anthu a mulungu anagonjetsedwa Kwambriri Ai chifukwa mmodzi wa iwo (Akani) anakwirira choipa mu nyumba yake. Mulungu anachita ndi anthu ake pankhani monga mudziwira. Tiyenera kumanga mpingo mu njira imene iyenera kumangidwira kuti tisakhale ndi nyumba yoonengedwa. Pamenepo pokha pamene anthu angochokere mu mpando wachiri kufika du mpando wachisanu.

Tithandizane ena kuti akule

Tsopano palinso fundo ina imene tiyenera kuti timango bwino. Izi zimakhuzana ndi (wampondo wachitatu) munthu wofooka, amene makhalidwe ake Sali abwino koma anapulumsidwa. Ngati tingamange mmene anthu anamangira miyambo ya anthu ndiye tingampaste uthenga kwa munthuyu. Tikuyetsesa kuti akhale mu zochita zathu. Koma ngati timange mmene anthu a dziko ndiye kuti zochita za munthuyo sizingadziwike ayi mwina ali kulira ndi chimo pamene agona usiku chifukwa mbusa amamva kulira kwa nkhusa ndipo ndi mkhristu woona okhala ndi mtima woona ndi mtima wofewa munthuyo safuna kukhala wogonjetsedwa. Ali kulankhulana ndi ndi Yesu za uchimowu, koma mu miambo ya anthu sathandizidwa ai amangomva uthenga ndipo amangoyetsa kwambiri koma nthawi zonse, uchimo umapititita kwa zaka mpaka amangosiya.

Pa dzanja lina, ngati tingamanga mnjira ya mulungu yimene iye anatiuza pali ndithu chiyembekezo. Mu nyumba ya mulungu munthu yemweyu pa nthawi yockepa pa sabata imodzi mwa mkhristu adzakhala ndi abable anayi kapena asanu amene ali kumuthandiza mu kufooka kwake. Ali kupemphera limodzi, ali kulankhula limodzi, ali kulankhula pamodzi mawu a Yesu. Ali kuulura machimo ake kwa anzake. Okhulupirira awa ali kuchengetana wina ndi mzake tsiku ndi tsiku ndi kubweretsa mphatso mu umoyo wa munthuyo. Choncho mmalo mwa kumva zowawa yekha, munthu wan’gono ameneyo ali ndi anthu amene ali okhudzidwa ndi moyo wake tsiku ndi tsiku kumuthandiza kusintha Palibe ali ndi chinsinsi mu umoyo wake kapena kutsiyanitsa moyo usadziwike ndi iwo amene amudziwa Yesu ndi kulumikizidwa kwa iye “kubatizidwa ndi mzimu

umodzi, mu thupi limodzi” Timathandizana mu zofooka sathu (monga ife tili nazo) palibe otchuka. Tikuthandizana wina ndi mzake monga mbale pakati pa abale.

Choncho tiyeni tinene za munthu amene ali mkhristu kwa sabata imodzi. Ali ndi chikhulupiriro mwa Yesu monga Messiah Baibulo limati machimo ake anasambitsidwa. Baibulo limati machimo ake awululika kwa iye mulungu ndi wokhulupirika ndi olungama ndi mwazi umapitirira kutitsuka. Chingachitike ndi chiyani ngati munthuyo atafa asanagonjetse uchimo mu moyo wake? Munthu uyu ndi opulumutsidwa ndi Yesu monga Paul wa Taitus ndi mwazi wa Yesu khristu munthu ndi wonulumutsidwa monga unatipulumutsa ife ku uchimo! Okhulupirira amakonda choonadi amafuna kusintha ndiye ndi opulumutsidwa, osati kungonamizira chabe. Ichi ndi chipulumutso chimene tili nacho abalendi alongo.

Uthenga wa bwino wa ufumu

Tikupatseni malembo amodzi amene amabweretsa zinthu zonsezi pamodzi mu buku la Ahebre Baibulo limati timakonzedwanso ndikukhala woyera. Ndinakonzedwanso-zinachitika pamene tinapeleka moyo wathu kwa Yesu. Kukonzedwa ndi kukhala woyera mawu oti “woyera” amatanthauza mbee ndikukhala wofunika kwa mulungu. Atate akonda mwana ndi onse amapeleka moyo kwa Yesu kuchokera mu mtima aika khristu ndi kubvala chikhristu .

Mwachocho mwana watsopano ndi mkhristu wakale onse ndi opulumutsidwa chimodzimodzi chifukwa atate anaombola mwana, Yesu ndiye pamene atate ayang’ana pansu ndi kuona anthu amene asambitsidwa ndi mwazi wa nkhusa. Angelo a imfa amapitirira ndipo sawakhudza ai mwazi wa Yesu wakhala wa thunthu kwa iye mu chionetsero cha mipando isanu amene anali mpando wachitatu, wachinayi ndi wachisanu. (Ana, atate ndi anyamata) onse ndi opulumutsidwa kwatunthu.

Ndi Yesu yekha amene ali wangwiro, mwamva? Ndiye pamene tabvala Yesu timakhala wangwiro ngati iye ali popitirira ndi chipulumutso chathu timakhala a ngwiro monga Yesu ali. Takhala a ngwiro ndi woyera ndi mmene malembo amatiphunzitsira. Ngati muli ndi mzimu mkati mwanu pamene muli opulumutsidwa kwenikweni ndiye mwakonzedwa mu ungwiro monga

Yesu ali. Ndipo machimo anu akhululukidwa ndipo dipo laperekedwa pa machimo anu onse ndipo ndinu okonzedwa mu mzimu wa Yesu.

Tsopano nkhani imene tikulankhula kulumukiza ndi mpingo mu maonekedwe osati kukhala wangwiro kokha komanso kukhala woyera-chida chothandiza mu nyumba ya mulungu ngati mpingo umangidwa mu njira ya mulungu monga ngati uyenera kumangidwira ndipo ndife okhunzidwa ndi ubale wa wina ndi mzake akhale wa ngwiro monga pakuti ali kale a ngwiro pa mwazi wa Yesu koma tidzawathandiza kuti akhale chida potumikira mulungu. Tidzawapanga a mphamvu mwa khristu. Tidzawapanga kuti akhale pa ubwenzi ndi Yesu ndipo ife sitidzapedza chipulumutso chokha kwa Yesu koma Yesu adzapenzanso kanthu kwa ife! Ana ang’ono kupedza kanthu kuchokera kwa Yesu Abambo ndi anyamata adzapereka kanthu kwa Yesu! Mwana wa nkhusa wa mulungu adzapedza phindu mzowawa zake.

Mpingo omwe Yesu akumanga ndi njira ya onse amene ali wokula msinkhu. Ngati timanga ndi miambo ya anthu, anthu ambiri amakhala makanda kwa nthawi yayitali. Izi ndi zokhumudwitsa Yesu mmalo mwa chisangalalo. Tikamanga monga mwa pulani ya mulungu ndi maonekedwe ake ndipo makandawo adzasanduka Asitifano, Paulo ndi a Yohane ndipo kuyambira wang’ono mpaka wamkulu adzakahala monga Yesu pamodzi ndipo mpingo udzakhala monga mzinda oikidwa pa mwamba pa phiri umene sungabisike. Pamodzi tonse monga mwa Paulo tidzakhala malo okhalamo mulungu mwa mzimu osati kungopedza mphoto ya chipulumutso chokha, koma tsopano pomalizira

Yesu adzapedza phindu la mpingo woota! Uwu ndiwo uthenga wabwino wa ufumu. Kukonzedwa ungwiro ndi kukhala woyera.

“Mulungu ndiye kuunika ndipo mwa iye monse mulibe mdima. Tikati tiyanjane ndi iye ndipo tiyenda mumdima, tinama, ndipo sitichita choonadi koma ngati tiyenda mkuunika monga iye ali, tiyanjana wina ndi mzake ndipo mwazi wa Yesu mwana wake utitsambitsa kutichotsa uchimo wonse”.

“Tikati kuti tilibe uchimo tizinyenga tokha ndipo mwa ife mulibe choonadi. Ngati tibvomereza machimo athu ali wokhulupirika ndi wolungama iye kuti atikhululukire machimo athu ndi kutisambitsa kutichotsa chosalungama chiri chonse.” (1 Yohane 1:5-9)

Alipo munthu amene akonda kuunika, ndipo wina amene amati alibe uchimo, koma akonda mdima kuchokera pa tsamba ili kuti mulungu amaona mosiyana.

“Ndikulemberani tiana popeza machismo akhululukidwa kwa inu mwa dzina lache. Ndikulemberani Atate, popeza mwamuzindikira amene ali kuyambira pachiyambi. Ndikulemberani anyamata popeza mwamulaka oyipayo ndikulemberani, ana, popeza mwazindikira Atate.” (1 Yohane 2:12-13)

Ngati timanga mu njira ya mulungu idzakhala yobveka bwino kwa iwo okonda kuunika adzachoka ku mwana kukhala atate ndi ku anyamata. Uwu ndi uthenga wodabwitsa!!

Kudzadzidwa Ndi Mzimu Woyera Pamodzi!!!

Lachiwiri la m'mawa a pa 5th October, 1999

Panthawi yokhala pamodzi mu Africa, kuthandizira m'chichewa, kutsiyana kwa malingaliro ndi zakumitima kwa abale.

Panopa, mbale amakamba za kukhonza kumva mau a Yesu abwino wokhala ndi Yesu kuti tikakhale akumva mau ake. Izi zili ndi zambiri zochita ndi ife pokhala kachisi wa Mulungu, pa idzi makhomo aku gehena sangatsekuke.

Baibulo likutiuzza zakudzadzidwa ndi mzimu woyela. Mzimu wa Yehova kukhala mwa ife ndi kutidzadza mpaka pa mathero. Ili ndi lamulo la Mulungu. Izi zithandauza kuti titha kumvera lamulo kapena ayi kuti tidzadzidwe ndi mzimu. Tikudziwa pokhala mkhristu, tayenera kukhala mwa Khristu, ndi kuti Khristu akhale mw aife. Amen? Choncho nkotheke kukhala mwa khristu, koma otsazazidwa ndi Khristu. Choncho nkotheke kutsamulingalira Yesu kapena kumumvela momwe tayenera kuchitira. Mwatsoka, ili ndi vuto la a Kristu ambiri lero. Koma pali vumbulutso lochokera kwa Mulungu za momwe izi zingatsithire. Njira yake ndi yokhuzana ndi kumanga mpingo bwino, “makomo a ku gehena tsangatsekuke,” tayenera kumanga miyoyo yathu kuti anthu a Mulungu, kuyamba kuchiyambi mpaka kumathero, kudzazika ndi Mzimu – osati tsogoleri awiri kapena m'modzi, koma anthu onse a Mulungu adzadzidwe ndi Mzimu.

Kuzamilatu

Ndingokuyambirani chinthuzi cha mfundo imeneyi. Tiyerekeze muli ndi ndowa ya madzi. Tinene kuti pokhala ndi ndowa ya madzi kapu ya madzi ili ndi chivindikiro pamwamba pake. Kapu ili ngati munthu yemwe ali ndi Yesu mkati mwake. Kwa munthu ameneyu kukhala mukhristu, wayenera kukhala mwa Yesu. Ndiye kapu yozaza ikhale mu ndowa. Ngati munthu ali wozazidwa ndi Mzimu, adzakhiliratu mwa Khristu, ngati

muli mphyeya mu kapu, idzakhala pa mwamba. Ngati sitili odzazidwa ndi Mzimu Woyera, ngati munthu, tayenera kukhala mwa Khristu ndi kupulumutsidwa, koma sitingaze mene mwa Yesu. Paulo alembera ku mpingo wa ku Agalatiya (Ch4), “Ndili mukuwawa wa kubereka mwana, pamene ndili pafupi kukhala ndi mwana. Ndikumva kuwawa kwa kubereka Yesu apangidwa.” Amalemba kwa anthu amu mpingo waku Galatiya amene adali wopulumutsidwa kale (zikunena za izi mu chapter 3:.. Mudali kufooka kwakukulu mu mpingomu, choncho. Tsadali khristu wokhazikika mwa iwo. Adali ndi mphyeya mwa iwo, pweya wa dziko, koma osati khristu. Sono adayanjana pamwamba. Iwo tsadazame mu mzimu wa Khristu. Chifukwa tsadali pawokha, wozazika ndi Khristu, tsadamire mwa Khristu.

Aroma 12:1-2 akutsindika kuti mwa kudziwa zabwino, chifuniro chabwino ndi changwiwo cha Mulungu kuti tumve Mulungu ngati munthu, tidzazidwe “Pantchito za dziko.” Titsakonde zomwe dziko limakonda. Titsakhale ndi malingaliro a dziko kapena kukhala monga momwe arankhulira. Tisithe manja athu mosiyana ndi a dziko. Timwaze ndalama mosiyana ndi momwe a dziko amamwazila nthawi yawo ndi ndalama. Mulungu anati kupembedza kwithu kwa uzimu kutsakhale ngati kwa dziko mu zovuta zilizonse. Mulungu adati kuti tikhale akusandulika, ngati kuchokera ku caterpillar kupita ku butterfly, mwa mau a Mulungu. Ndiye tikhoza kumva Mulungu “Ndiye tikhoza kudziwa zabwino chifuniro chabwino ndi changwiwo cha Mulungu.” Ngati tili ndi zina zamudziko mwa ife, m'malo mwa kusandulika kwa mau a Mulungu, tidzayanjana pamwamba. Ngakhale tingakhale mwa Kristu ndi ku pulumutsidwa, sitili ozama mu cholinga cha Mulungu.

Tikufuna M'odzi ndi Nzake

Cholinga cha mpingo ndi chothandiza aliyense kudzazidwa ndi Mzimu Woyera, sono tikhoza kuthandizana kuchotsa dza mudziko mu miyoyo yathu. Ku Hebrews 3 akuti, “Tayenera kuuzana ndi kuthandiza ndi kuchenjezana wina ndi mzache tsiku lililonse kuti patsakhale modzi mwa ife amene adzachite manyazi ndi kukanidwa. Baibulo likuti tiyenera kuthandizana tsiku ndi tsiku. Tichoke mumanyumba mwathu ndi kulowa mumiyoyo ya ena, mu malo ogwilila ntchito ndi mu ma nyumba

mwa azizathu. Tayenera kuthandizana kuti tisakhale adzichito chito za dziko. Anthu ena mati, “ndili ndi ubale wawo ndi Mulungu wawo.” Izi sizomwe Baibulo likunena. Baibulo likuti “langidzanani wina ndi zache kuti pasadzakhale okanidwa ndi wotsalandilidwa.” Baibulo likuti ndife a nsembe awokhulupirira ndipo tayenera kuthandizana wina ndi nzake kuti tikazazidwe ndi Mzimu Woyera. Timagwiritsa ntchito mphatso zomwe zili mkati mwa ife kuthandiza ena kuti adzaze ndi Mzimu Woyera. Membala wina aliyense wa mpingo athandize membala nzake kumpingo.

Izi ndi zinthu zosiyana momwe Anthu ambiri pa dziko lapansi amangaira pamodzi cikhristu. M'mayiko ambiri, anthu amabwera pamodzi pa tsiku la sabata ndi pa misonkhano. Momo amakhala ndi “Mumpingo yambiri padziko la pansu kulibe kuti dziko liti, Anthu amabwera pamodzi pa sabata ndikukhala mumizele. Ndiye akulu .--- akulu (anthu oyera) amabwera kumbuyo kwa anthu ndi kuyambitsa mapologalamu. Koma izizi simomwe Baibulo limanenera ayi kuti cikhristu cimakhallira choncho. Tili nayo, mmayiko yosiyana siyana, momwe tamangira mpingo molakwika mudzankha zoposa tusauzande (2000) mdzaka zapitazo.

Chifukwa chiyani tamanga molakwika mpingo chonchi? Chifukwa mamangidwe ache amangidwa ngati a chipangano cha kale, momwe akulu a sembe ali momo ndipo anthu ambiri ali momo kuwonerera. A Levi (wasembe) amapeleka sembe za anthu onse. Iyeyo amakhala mu nyumba ya Mulungu wa padera dera amene amawathandiza anthu kuti amudziwe Mulungu. Ichi ndi chabwino ngati inuyo munakhalapo zaka thusauzande (2000) kumbuyoku ngati ife tifuna kukhala a Kristu osati Ayuda, ndiye timange ngati Akhristu AMEN? Tamanga molakwika chikristu mumayiko wosiyanasiyana koma, Mulungu alikubwezeretsa tsopano mpangano la tsopano Mchikristu mudziko lonse la pansu.

Ufumu wa Ansembe

Mpangano la tsopano anthu onse a Mulungu ayenera kukhala a sembe kwa wina ndi mzake. Chikumbu kumbu cha Mulungu si cha kuti munthu ozozedwa modzi azilamulira mapologalamu ayi. Mawu a Mulungu akunena kuti Yesu anakwera kumwamba mwamba ndipo anapeleka zipatso pa anthu ake, anapanga ufumu wa ansembe. Iye anayika gawo limodzi la iyi mwini pa anthu ake kuti iwo ndi woona osandulika ang'ono ndi akulu.

Ndi chifukwa chake amafuna mphatso ya wina ndi mzake. Timafuna mphatso zonse Yesu. Pali mphatso zambiri – mbiri chifukwa zonse Yesu anadzithira pa banja lake (mpingo). Ichi ndi chifukwa chake Yesu anati, tonse tili a mbale wina ndi mzake sitifuna ife, mtundu modzi kapena mphatso yimodzi yizimilira patsogolo pathu nthawi zonse. Izizi sitizalora kuchitika pakati pathu. Onse amene osindidwa oona ake ndipo okhala mkati amakhala a kulimbika mmoyo wawo nthawi zonse kwa wina ndi mzake ndipo kuwonesetsa (Aheb 3:12-14) kuti onse ndi a sembe.

Mtima wa Mulungu, mpatso yanu yikale yanga komanso mpatso yanga yikhale yanu. Yesu amatero, “Musamuche wina mw ainu wamkulu, Revelande, Mbusa, kapena wasembe” ngakhale kwa ophunzira ake aja asanu ndi awiri, iye anati “inu nonse muli a mbale,” ngati chiri choona kwa Petulo ndi Yohani nditi ndi choonadi kwa ife tonse Amen. Mphatso zimene zili mkati mwa ambale ndidzo gawo la Yesu. Ngakhale ana ali nadzo mphatso zimeneso ndi gawo la Yesu. Mphatso zonse zimafunika pa moyo wathu. Ife tonse ndife ambale. Izi ndi zomwe Baibulo limanena.

“Inde lero a mbale, ngati mumbwera pamodzi, pali wina ali mawu achiziwiso, yimbo, kapena vumbulutso,” izizi ndi zomwe kawiri kawiri mawu a Mulungu amanena ku 1 Akorinto 14, “Ngati mumbwera pamodzi, ambale, aliyense ali ndi mawu a chiziwitso, yimbo, vumbulutso kapena uneneri.”

Ngati timakhala choncho, ngakhale osakhulupirira amagwera pamaso pake ndi kulira, nanena, “Mulungu ali pakati panu.” “Ngati vumbulutso lavumbuluka kwa munthu wa chiwiri ndiye WOYAMBA ASIYE NDI KUKHALA PANSI!” Ichi chi ndi chimene chimathandauza ku 1 Akorinto 14. izi zisimaoneka kawiri kawiri ndi amanena “amakonda kukhala oyamba, amakonda kukhala olamulira komanso kuonesetsa ngati “iwo ndi auzimu eni eni. Ndi kutenga ndalama za oyera mtima.

Ife tiyenera kukhala ufumu wa a sembe. Ife tiyenera kumangilidwa wina ndi mzake tsiku liri lonse. Ngati sitimangirilana, Baibulo likuti tizaumitsidwa ndi kunamidzidwa. Chikumbu kumbu chathu chizamangiriridwa. Ife tidzazakhala kuyerekedza! Kutengeka ndi zinthu zonse zimene zimaoneka zochimwa kumoyo wanthu. Ngati sindingapeze anthu ambiri ozipeleka otsatira a Yesu kukhudziwa ndi

moyo wanga tsiku ndi tsiku ndi ena Sali okhudzidwa ndi moyo wanga ndiye kuti tidzakhala ounotsidwa mitima ndipo sitidzadzidwa choonadi. Izi ndi zimene Baibulo limanena nthawi zonse. Tiyenera kukhala mu moyo pamodzi kuthandizana tsiku ndi tsiku. Ngati mukufuna kutsutsa baibulo ndi kunena kuti siloona, ndiye kuti mudzayamba chipembedzo chanu. Anthu ambiri ali mu chipembedzo chotero. Koma nonse a inu mwasonyeza pa kuzipeleka kuti muchita chilichonse cha Yesu. Choncho tiyeni tipite kukwera pamodzi ndi iye tsopano!

Tsiku Lililonse

Yesu akumanga mpingo wake umene makomo a ndende sadzaulaka. Yesu akubweletsa mphatso kuchokera kwa anthu ake ndikulora iwo kuti akhale ansembe tsopano – osati msonkhano, koma tsiku ndi tsiku. Baibulo limati ululani machimo kwa wina ndi mzake ndi kupemphererana wina ndi mzake kuti muchilitsidwe. Tadikilani kodi anthu onse a Mulungu amachita zimenezi? Ndi liti lomaliza kuwulura machimo anu kwa mbale kapena mulongo. Kodi mukufuna kuchilitsidwa? Kodi mukufuna mphamvu ya Mulungu mu moyo wanu? Baibulo limati lapani machimo anu kwa wina ndi mzake. Chifukwa chiani sitipanga? Sitipanga izi kwa nthawi zonse chifukwa timaopa. Sitipanga chifukwa cha miyambo ya anthu imene yatimeza ife. Taleka kukhala woyenerera chifukwa cha kuzikonda. Mulungu akuti kwa inu ndi ine. Titsegule mitima yathu kukhala ozichepetsa ndi wofewa. Kuwulura machimo kwa wina ndi mzake tsiku ndi tsiku ndi kupemphereana kuti tichiritsidwe.

Iyi ndi imodzi imene timathandizira wina ndi mzake kudzazidwa ndi Mzimu Woyera. Timatsegula mitima yathu kuchengetana wina ndi mzake tsiku lililonse. Tsiku ndi tsiku kuti pasaoneke wowumitsa mitima kapena kunyengedwa. Atero Ambuye, Mulungu wanena kuti tiyenera kutsegula moyo wathu kwa wina tsiku ndi tsiku, tsiku lililonse ngati tizamanga munjira yotere yokumanirana pa Mulungu ndiye kenaka tipita ku nyumba zathu ndi kukhala mosiyana ndi mabanja. Tidzakhala osamvera Mulungu.

Mulungu walankhura momveka bwino pamene tingayendere pamodzi ndi kuthandiza wina ndi mzake kudzozedwa ndi Mzimu Woyera. Mulungu

anati, “thandizanani wina ndi mzake tsiku ndi tsiku.” Mulungu anati, “Tikuika mzimu wanga ndi mphatso mkati mwa inu ndiye taya moyo wako chifukwa abale tsiku ndi tsiku.” Mulungu anati, “lapitsanani machimo anu kwa wina ndi mzake tsiku ndi tsiku.” Mulungu anati, “Tengelelani zothobwetsa ndi kukwaniritsa lamulo la Kristu.”

Muntha kuona kuti ndi chinthu chochitika tsiku ndi tsiku. Mungatenge bwanji zobvuta za munthu wina mu msonkhano kukwaniritsa lamulo la Ambuye tiyenera kutengelana zobvuta za munthu wina. Nanga zothodwa zimenezi zili kuti? Kodi zili ku misonkhano wa Mulungu? Ai, zobvuta zamoyo zimapezeka ndi ana athu, ndi akazi athu ndi amuna athunso mu zintchito zathu. Zobvuta zamoyo ndi pamene chisilamu kapena chipembedzo chonama ndi mabanja athu a thupi atida ife chifukwa choti tabwera kwa Yesu. Amaswa moyo wathu ndipo sitidziwa chimene tingachite. Tikufuna inu kuti mundithandize mabvuto anga pamene mwana ali odwala. Sindifuna kumva uthenga wako lamulungu singapite kumeneko pamene mwana wanga adwala. Sindifuna kumva nzeru wako yozama ndi kulankhura kozama ngati sungathe kundithandiza pamene ndili ndi mabvuto ndi mkazi wanga. Ndi chochitika tsiku ndi tsiku sizokhudza misonkhano ai. *Kutengelana zothobwetsa tsiku ndi tsiku ndi kukwaniritsa lamulo la Kristo.*

Tamanga molakwika mpingo mu mayiko ambiri kwa zakanso zambiri. Mulungu ali kuitana tsopano anthu amene ali ndi kulimbika ndi kuzichepetsa ndi kuzipeleka yekha kuti imangidwe bwino. Ngati tidzamanga nyumba ya Mulungu kusata maonekedwe amene anaikidwa. Makomo a ku Hade imene ndagwira. Mudzachita, Atero Ambuye. Tikaona monga Yesu pamene adali kuno. Yesu sanangokamba chabe ai. Anakhala moyo Yohane 1 amatero “Moyo ndipo unasanduka kuunika kwa anthu.” Ndi chonchoso mpaka lero moyo wa tsiku unasanduka kuunika kwa anthu. Ngati tikufuna anthu kuti aone chikondi cha Mulungu ndipo ngati tifuna kuti abwere kwa Yesu mmalo mwa ndalama ndi mphamvu ya chisilamu, ngati tikufuna kuona anthu ndi kunyada kwawo. Tiyenera kukhala mu moyo wa Yesu pamodzi tsiku ndi tsiku.

Mbali ya Aliyense

Talankhula zokhala ngati kapu ya madzi yodzadza ndi kulowa mwa Yesu. Tingalankhulenso za chinthu mpika wa mbatata ndinso mapika wa chimanga chosatongola umu ndi mmene tamangira mpingo kwa zaka 2000 zapitazi anthu amabwera onse pa lasabata monga anthu okhala ngati mbatata kapenanso monga chimanga mtima wa Mulungu suli mu mphaka wa mbatat kapenanso aliyense payenkha mu mphaka pamodzi kwa masiku awiri limodzi, kapena atatu pasabata. Pokhala mu nyumba mnalowa chipembedzo mopembedzelamo si mwabwino ngati sitingathe mitima yathu ndi mmene tingagwirile wina ndi mzake tsiku ndi tsiku. Msonkhano pawokha sumangitsa kuti ndi mpingo wa mbaibulo ai. Uku ndi kumene mbaibulo amati malo ophunzitsilamo mphika wa mbatata pa yekha payenkha si mpingo. Mungathe kuponya mbatata zonse kapenanso zimanga zonse mu mphika lamulungu lililonse komabe sukhala mpingo simpingo ai. Mpingo woona umafanana ndi mphika wa mbatata zosenda ndi chimanga chosendedwa ndipo simakhala zofanana. Monga zimodzi mongaso okhala amodzi mu chikhulupiriro. “Mtima umodzi moyo umodzi, onse pamodzi ndi machitidwe amodzinsu. Angakhale ndife ambiri koma ndife mmodzi kubatizidwa ndi Mzimu mu thupi limodzi pamene wina sanganene kwa mzake sindifuna iwe mpaka nthawi yina sabata ya mawa.

Mphika wa mbatata yosenda kapenanso chimanga ndi moyo wanu kukhala mbali ya mbali ya ine ndi moyo wanga kukhala wa ine. Pamene til amodzi monga Yesu ndi Atate ali – pamenepo ndiye mpingo wowona ena angapulumsidwe inde popanda moyo umenewu koma sakupindula kwa Yesu pa msonkhano. Powonetsera kudziko za mphamvu yake ndi moyo. Ndidzamanga mpingo umene makomo a ndende. Sangathe kuwononga! Pokula msinkhu, kwa ana ndi akazi anu ndinso okhala nawo pafupi ndi ena olumikizidwa ndi kulukidwa pamodzi. Umenewu ndi mpingo mu pulani ya Mulungu.

Pamene moyo wanu uli mbali ya moyo watsiku ndi tsiku pamene mphatso yanu uli mbali ya ine ndi mphatso yanga ndi mbali yanu tsiku ndi tsiku. Pamene ndiulura machimo kwa inu ndipo mukuulura machimo kwa ine ndipo tipemphererana wina ndi mzake kuti tichilitsidwe. Pamene mundidziwa ine koposa choncho mungathe kuwona kuchokera mu maso

anga kuti ndawaidwa moyo ndipo muli kunditengera zothodwa – *Ndi pamene mpingo udzayamba kukhala mpingo wa Yesu*. Yesu anati umu ndi mmene (Asilamu, Amboni za Yehova, Amarmorori ndi onse wofooka ndi othentha chabe mu chipembedzo) adzadziwa kuti chikristu ndi chochokera ndithu kumwamba. Onse adziko adzadziwa kuti tili a iye pamene tikondanilana

Mungathe kunena za mwazi wa Yesu ndi mau a Mulungu koma mpaka mutayamba kukhala ndi moyo wokondana wina ndi mzake ndiye kuti odzangokhala mau chabe. Ngati dziko lidzaona ife kukondana wina ndi mzake chifukwa choti moyo wathu wataika pothandiza wina ndi mzake ndiye kuti moyo wa Mulungu ndi mphamvu idzakhala ya mphamvu koposa. Mukumizidwa ndi mu mphamvu (ndipo tidzapachitikidwa ndi kudedwa, kunamizidwa monga mwa Yesu analankhulira!).

Atate akonda mwana ndipo tidzayamba kuoneka monga mwana kuwala monga nyenyezi zakumwamba. Mudziyikidwa pamwamba pa Phiri umene sangathe kubisika. Ameneyo ndiye Yesu ndi cholinga cha mkwatibwi wake, mpingo sitingoyenera kukhala owonera chipembedzo ndi kunena mau ena tiyenera kusiya kukhala mu mipando monga zidoli kumvetsera kwa wina ali kulankhura. Tiyenera kuti tikhudzidwe kwatunthu mu miyoyo mozama ya azanthu tsiku ndi tsiku abale pakati pa abale. Izi simsonkhano okha koma kupeleka mitulo kwa ine ndiponso ine kwa inu tsiku lililonse mu zinyumba zathu ndi muzintchito kumunda ndi kubanja athu izi zimafunika kusintha mmene mumagwilitsira nthawi yanu ndipo musinthe zinthu zimene munazitenga kuti ndi zoyambilira mu moyo wanu ndi kutero *“Thangani mwapeza ufumu wa Mulungu.”*

Banja Lenileni!!

Yesu anati ngati mupeleka moyo wanu ndi kukhala mkristo mudzakhala ndi amai ambiri abale ambiri ndi alongo ochuluka kuthandauza kuti mgwilizano wopambana ndi zimene baibulo limathandauza za chikristo! Mudzakhala ndi chiyanjano amene ali pafupi monga mai ndi mwana kapena mbale ndi mlongo pamodzi pafupi – pafupi molumikizana chibale. Sanati abwenzi ambiri kapena otizungulira ambiri Yesu anati mpingo ndiwo zana la mgwilizano umene uli olumikizana monga mai kwa mwana wake.

Mai wabwino amamva kulira kwa mwana wake ndipo amamva kulira kwa mwanayo pamene wabvulala kapena pamene ali ndi njala. Awa ndi kulira kosiyana amadziwa kulira kwa mwana wake molumikiza – zonse zokhudza za mwana wakeyo. Yesu anati mu mpingo wanga woona mudzakhala ndi ubale ochuluka “wolumikizana mongaamai ndi mwana mudzatha kuwona mu maso anga, ndinso ndizatha kuwona mmaso mwanu pamene mwatopa muli ndi njala, mwakwiya ndi pamene odandaula izi siza msonkhano ai sichoncho kodi? Siza lamulungu mmawa mukulalikira, sinchoncho kodi? Simsokhano wolalikidwa lamulungu mwamva kodi? Koma moyo wa tsiku ndi tsiku pamodzi monga amai ndi mwana wake.

Mai kodi angakhale ndi mwana wake lamulungu lokha basi akhoza kukhala mai oipa, sichomwecho? Chidzachitike ndi chiani ndi mwanayo? Mwanayo adzafa. Izo ndi zimene zachitika ndi akristu ambiri tamanga molakwika kwa nthawi yaitali ndi munthu olalikira ndipo ena tonse kumangomvetsera ndi kumaimba ndi kuvina ndi kupita kumudzi ndikukhala ndi moyo wosiyana chifukwa cha ichi ana ambiri afa ndipo amai ambiri asweka mitima yawo.

Cholinga cha Yesu pa mpingo wake ndi kukhala amai ambiri abale ambiri ndi alongo ochulukanso. Malo athu ndi zokhala nazo ndi nthawi ndi ndalama sizathu ayi, ifenso si a ife tokha. Tinagulidwa ndi mtengo wamkulu ndi mwazi wa Yesu ndiye timapanga chiganizo kuti tisankhalenso ndi moyo wathu pokhala mu moyo wa wina ndi mzake tsiku ndi tsiku AAH ndatopa ndikuganiza zopita kukagona Ai pita kukakumana ndi kukonda ambale ako gwira ntchito pamene kuli masana usiku ubwera ndipo palibe chochita. Ndikuganiza zochita zimene ine ndizikonda. Bweletsani mbale kwa ine ndi abale enanso ambiri chitani ndi anthu ena chabwino tiyenera kupita ku msika. Ndilibwe nthawi yokhalira ndi abale kapena alongo atengeni onsewo. Ndipo chitani nonse pamodzi ndipo mumodzi. Ndipo njiramo mudztha kudziwa zosowa za zimene afuna ndi zinthu zimene zili zofunika kwa iwowo chifukwa ndinu okhuzidwa ndi moyo wanu ndipo sika ndi muzochita osati mphatso yathu yokha imene ili yokha-yokha. TONSE tili ndi mphatso ya Yesu ndikuonetsera moyo wake. mngelo anati “pitani nonse ku misika ndi kuuza wina aliyense za moyo wa TSOPANOWu umene muli nawo wa Yesu! Izi ndi zimene anthu onse

adzadziwa. Pakuona kuti muli KUKONDANA WINA NDI MZAKE!” moyo unakhala (ndipo unakhala) kuunika kwa anthu.

Ngati tidikira mpaka kutha ntchito yathu yonse ithe kuti tikhale banja, sitidzakhala banja. Banja limapanga zinthu zonse pamodzi. Kuchapa zobvala zathu pamodzi ndi kupita ku msika pamodzi. Kuyenda pamodzi ndi kulankhura machimo kwa anthu za Yesu. Pamene tili tonse pamodzi timaulura machimo kwa azanthu timati, mlongo mungathe kundipemphelera? Ndili wotopa ndi ana anga ang’ono ndiponso ndakwiya ndi mwana wanga wa ng’ono dzulo. Ndafunsa Mulungu kuti andikhululukire komanso ndikufuna kuti andikhululukirenso kapena mb’ale kodi mungakhululukire di kundipemphelera ndinali ku ntchito ndipo ndinakwiya ndi wina amene amafuna kundinamiza ndipo ndinalankhura mau oipa kwa iye. Ndinapita ndikumufunsa kuti andikhululukire ndipo ndili kuwulura machimo anga pa iwe. Choonde mungathe kundikhulukira ndi kundipempherera ndikuti ndingakhale olimba zonse. Inde ilipo nthawi imene timafunika kukhala patokha ndi kupemphera mu seri ndi kukhala ndi nthawi ya wekha ndi zinthu zina. Koma pena pake tataya moyo wa Yesu umene umatikhalitsa pamodzi. Mphaka Yesu anatenga abale atatu ndi iye pamene anapita ku Geshemane mmunda uja pa nthawi yowawitsa ya moyo wake. ndi ifenso tichite choncho. Aliyense amene amati ndi wake wa iye ayenera kuyenda monga iye anayendera ndi chabwino ndi chopambana chimene chataika mu njira ya makona mu nyengo ya kutanganidwa Nu Clear. Kuzikonda ulesi ndi kunyada. Tiyeni tilengeze Yesu kuti dziko lidziwe ndikuti tikule msikhu.

Titsegule Mitima Yathu

Ichi ndicho chifungulo chenicheni. Ife tiyenera kutsegula mitima yathu ndikulora anthu ena alowe m’mitima yathu. Ichi ndi chofunikira kwambiri. Palibe njira ina yozungulira ichi. Ife tiyenera kutsegula mitima yathu kwa wina ndi mnzake kuti Yesu akhonze kulowamo ndipo abale ndi alongo athu akhonze kulowamo. “Ufumu wa Mulungu siuli pano kapena apo,” Yesu adatero “Ufumu wa Mulungu uli mwa inu.” Ngati inu ndithudi mufuna Ufumu wa Mulungu, sikungokhudza kukhulupirira zinthu zoonza kapena kupita ku misonkhano. “Ufumu wa Mulungu siuli pano kapena apo; uli mwa inu.” Ichi chitanthauza kuti ine ndifuna Ufumu wa Mulungu,

ndiyenera kulowa mwa inu ndi mmene Ufumu wa Mulungu uli. Ichi chitengera kulimbika mtima, kudzichepetsa ndi kumvera. AMEN? Ife tiyenera kukhala osakanizana osati osiyana. Ife tiyenera kukhala zana la amai, alongo ndi abale – osangoti zana la abwenzi abwino.

Ngati ife tidzayamba kukhala munjira iyi kwambiri ndi kwambiri tsiku lililonse pamodzi ----- ngati ife tidzatuluka m’nyumba zathu ndi kulowa mumitima ndi miyoyo ya anthu ndi kuwalandila iwo m’mitima ndi miyoyo, ndiye kuti ife tidzaona mpingo moti makomo a ndende sadzaulakanso konse ayi! Ife sitidzafuna zigawo zonse zongopangilapozi za Baptist, Pentekositi kapena Nazarene. Ife sitidzafuna zigawo zonse ayi *chifukwa Yesu adzadzadza ife!* Ife tidzaona ulemerero wa Mulungu ukutsika mu miyoyo yathu munjira yodabwitsa. Ife sitifuna zizindikiro zonse izi tsopano.

Tsopano anthu adzadzidwa ndi mzimu Oyera onse a iwo, ndipo ife tidzamizidwa pamodzi mwa Khristu.

Ife taona zotsekeredza izi zikugwetsedwa pansu mu malo ambiri. Mpingo umene ife tili mbali uli ndi anthu ochokera kwambiri za umoyo zosiyanasiyana zambiri amene ayika mbirizo pambali chifukwa choti agwa m’chikondi ndi Yesu, pamodzi, ndipo ife tili kuthandizana wina ndi mnzake kukhala kukhala ngati iye tsiku lililonse. Khalani ndi masomphenya awa pa mzinda wanu. Yesu afuna anthu AKE kuti akhale AMODZI. Ife sitikhala amodzi chifukwa tapanga chisankho kutaya ziphunzitsa zathu. Ife tidzakhala amodzi pokhapokha pamene tapanga chisankho kutaya machimo athu. Sikuti ndi aliyense AFUNA ichi – koma INU mukhonza kukhala kapena kufa chifukwa cha icho!

Ufumu Kulandidwa Zida?

Tangoyeserani padali mafumu awiri – mfumu yabwino ndi mfumu yoyipa. Mfumu yabwinoyo idali ndi mphamvu kwambiri kuposa mfumu yoipayo. Ankhondo a mfumu yabwino adali ndi zida zimene zikadagonjetsa mfumu yoipayo. Zida izi zidali za mphamvu yoposera. Mfumu yoipayo idadziwa kuti siyingaime kulimbana ndi mfumu yabwinoyo. Tsono mfumu yoipayo idaitanitsa msonkhano wa akulu ankhondo ake.

Iye adati, “ine ndili ndi njira zitatu.” Ife sitingalimbane ndi zida izi, tsono tiyeni choyamba tinyengerere gulu la nkhondo la mfumu yabwino kuti

iwo safunika kuphuzira kumenya nkhondo ndi zida zao. Tiyeni tipange iwo azingokumana pamodzi ndi kungoyankhula zokhudza zida zao. Atsogoleri awo akhonza kuyankhula zokhudzana ndi kudabwitsa kwa zida zao. Iwo azimva bwino zokhudzana ndi zida, koma iwo ayiwala za mmene angadzigwiritsire ntchito izo.”

“Nayi njira yanga ya chiwiri. Ife tidzagawa gulu la nkhondo la mfumu yabwinoyo. Ife tidzazala mbeu ya chigawanikano pakati pao. Tsono kenako, mmalo mwa gulu la nkhondo limodzi, iwo adzakhala ndi timagulu tating’ono tokwana zana limodzi. Iwo sadzadziwa m’mene angamenyere nkhondo pamodzi. Ife tidzawagawa iwo ndi kuwagonyetsa iwo.”

“Nayi nira yachitatu. Ife tidzanyengerera gulu lankhondo la mfumuyi kuti alore wina aliyense kulowa nawo gululo. Ife tidawauza kuti gulu la nkhondo lalikulu ndi laulemerero ndikuti aliyense amane ali ovomera kuvala uniform akhonza kulowa nao. Ife mwachinsinsi tidzatumidza ena mwa asilikali kukalowa nawo gululo. Motero, iwo adzakhala ndi zida zamphamvu koma sadzadziwa kugwiritsa ntchito iwo adzakhala ogawikana pa wina ndi mnzake. Ndipo gulu lao lidzadzaza ndi anthu amene ali opereka ulemu kwa ine, mdani wao.” Munjira iyi, mfumu yoyipa idali ndi kuthekera kolimbana ndi mfumu yabwino.

Umu ndi mmene zachitikira mu mpingo. Nyimbo zili bwino, monga momwe tayimbira – Mwazi wa Yesu siudzataya mphamvu zake. Mau a Yesu sadzataya mphamvu zake. Dzina la Yesu silidzataya mphamvu zake. Izi ndizo zida zathu. Satana angayime kulimbana ndi Dzina, mwazi ndiponso Mau a Yesu. Koma mpingo wa Yesu wataya mphamvu zake. Mmalo mwakukhala akhulupirira a unsembe, ife tasanduka omvera ndi ochita a ndondomeko (pologramu). Ife tayiwala mmene tingagwiritsire ntchito Dzina la Yesu, Mwazi wa Yesu ndiponso Mau a Yesu. Ife tili okhutitsidwa ndikungokhala pamodzi ndi kumamvera kwa wina wake akuyankhula zokhudza zinthu izi. ife tilinso ogawikana wina ndi mnzake. Pali mazana a mipingo, wina uliwonse ndi miyambo. Ife talola migawanikano iyi kuima mnjira yathu ife tisagwirizane pamodzi ndi kumenya nkhondo ndi mdani. Ife takhalanso auchisayero. Anthu ambiri mmabwalo achipembedzo samudziwa ngakhale Yesu monga Mpulumutsi ndi Mbuye wawo. Iwo ali osokonezeka. Iwo akuganiza kuti amamudziwa Yesu, koma iwo siali choncho ngakhale pang’ono, chifukwa iwo sadapereke moonadi miyoyo yawo kwa iye.

Umboni Wa Moyo Wa Yesu

Tsono mu mnjira zonse izi mpingo watwya mphamvu zake koma Yesu adanana kuti mpingo umene iye amangaudzakhala wakutheker kugonyetsa makomo a ndende. Chimene ife takhala tikuyankhula lero ndi yankho la vuto ili. Ngati ife timanga mnjira ya Mulungu, ife tidzakhala woyera. Osati chifukwaife tili a bwino, koma chifukwa anthu ambiri akutithandia ife tsiku lililonse. Iyi ndiyo njira ya Mulungu, Ngati ife timanga mnjira imeneyi, ife tidzayanjanitsidwa mu umodzi. Ndipo ngati timanga mnjira iyi, membala aliyense adzagwiritsa mphatso yake pochitira ubwino onse. Ife sitikhala womvera chabe, ife tidzakhala asilikali, ndipo Banja la chikondi. Banja loona, kutengera kwa Yesu mu Marko 3:33-35 iyi ndiyo njira imene mpingo wa Yesu ukhonza kutengeranso mphamvu zake.

Ife tinakwera kuno mumatola mmawa uno. Oyendetsayo aamanena, mukuwawa, kuti chisilamu chakhala chikutenga mphamvu mu dziko muno. Chabwino, ine ndekha sinditsamala kuti wina ali ndi nambala yambiri. Chimene ine nditsamal ndi choti, padzakhala umboni wa Yesu khristu pa dziko ili. Umboni womwe ndi woyera, umene ndi wa mphamvu ndi umene uli ndi mphamvu yogonyetsa satana mmiyoyo ya abambo, amayi ndi ana. Ichi chikhonza kuchitika pokhapokha ngati mpingo wa Yesu ungatengeso mphamvu zake. Ife tiyenera kuthandizana wina ndi mzake. Ife tiyenera kumanga miyoyo yathu pamodzi, tsiku lililonse. Ngati ife tizakhala mnjira iyi, diye kuti dzina la Yesu lidzatengedwa mu ulemu wa pamwamba. Anthu adzayamba kunena kwa ife, “Tiudzeni ife za Yesu ameneyu amene inu mumudziwa”. Apa ndipo pothera pathu, ngati ife tidzakhala ndi kulimbika mtima kuti tiumange njira iyi. Ameni?

Chotsani Dengu Pa Chomera

Aheberi 3 amanene kuti ife tiyenera kulimbikitsana wina ndi mzake tsiku lilonso. Ife tiyenera kuchenjedzana wina ndi mzake tsiku lilonso. Ife tiyenera kuthandidza wina ndi mzake tsiku lilonso ndi ana athu ani akazi athu ndi ntchito zathu mminad mmisika----kutithandizana winw ndi mzake siku lilonnse. Aheberi 3 amatiamapitilira kunena kuti ngati ife sitipanga achi, ndiye kiti dzinthu ziwiri zichititka. Ife tidzasanduka ouma, ndipo ife tidzaputsidwa. Ngati inu muli ndi chikho cha madzi ndipo mukuthira madziwa pa nthaka yofewa, nthaka yofewayo imamwerera

madziwo. Koma mukathira pa mwala youma madziwo amangoyenderera pa mwamba. Nthaka ndi yofewa ,mwala ndi wouma. Mwala ndi wouma sungalandire. Ngati ife sitikhalirana ndi wina ndi mzake tsiku lilonse monga Aheberi 3 afotokonzera, ife timauma. Mau a mulungu, sangalowe mmtima yathu, iwo sangalowerere. Mtima wathu watsanduka ouma.

Ife tidali chabe mdzinda wina wantunda wokwana milingo zana limodzi kuchoka pano, pafupi ndi nyanja. Nthaka ya mfupi ndi nyanjayo ndi yofewa, chifikwa madzi nthawi zonse ali pa iyo. Kutali ndi nyanjayi, nthakayi siiyandira mvula yambiri ndi youma. Ife tiyenera kukhala mwa wina ndi mzake tsiku lililonse kapena ife tiuma. Ife sitingamve Mulungu. Ife sitingakule. Ngati inu mutenga chomera ndikuyika pansu pa dengu, chomeracho chidzafa. Chomera chimafuna kuwala. Monganso ife!n kuwerenga ma Baibulo sikokwanira. Kukhala nawo mitsonkhano pa sabata sikokwanira. Monga mbewu pansu pa dengu, ife tikhodza kufa. Timafuna kuwala. Pamodzi tikhala mnjira iyi. Ife timagawirana kuwala pa wina ndi mnzake. Popanda kuwala kumeneku, tifa. Popanda kuwala kwa wina ndi mnzake mu miyoyo athu tsiku lililonse, ife timauma.

Chinthu chachiwiri chimene chimachitika ndichakuti, ife timaputsitsidwa. Ichi chitanthauza kuti sitidziwa kuti ife ndiouma. Ife taputsitsidwa. Ife tikuganiza kuti tili ofewa, koma ndife ouma. Ife timakonda kuyimba ndipo timakonda nthano za mBaibulo. Ife tikhozanso kukonda kuyankhula zambiri zokhudza Yesu. Koma ife tili ouma ndipo ife sitikudziwa ichi, chifukwa abale samatithandiza ife kukhala ofewa tsiku lililonse. Ichi ndi choopsa kwambiri! Ngati munthu ali wakhungu, koma iye aganoza kuti ndi ondetsa wabwino wa basi, sichoncho?! Icho ndi choopsa!

Munjira yomweyo, ife tikhoza kuputsitsidwa. Popanda kuwala kwa anthu a Mulungu mu miyoyo yathu tsuku lililonse, sikuti tidzangouma kokha ayi ife tidzaputsitsidwa. Ife sitidzaona mbali immene ili mwa ife imene siili ngatiYesu. Malingaliro athu adzaputsitsidwa. Awa ndi malo oipa kukhalapo. Kuwala kwa Mulungu sikungalowe, ndipo zinthu zoipazo sidzingachuluke. Ife sitidzawadziwanso kuti zinthu zoipazo zilimo, chifukwa ife taputsitsidwa. Ngati inusimukhalira tsiku liri lonse pamodzi ndi wina ndi mnzake mu njira imene Baibulo limafotokozera, ndiye kuti inu ndi ouma ndi oputsitsidwa. Ichi ndicho Baibulo linena. Mulungu sanama ayi. Aliyense amene sakumanga tsiku ndi tsiku pamodzi ndi

anthu ena, ndi mau a Mulungu, amauma ndi kuputsitsidwa. Ngati ife tidzadandaulirana ndi kulimbikitsana wina ndi mnzake tsiku ndi tsiku, mitima yathu iodzafewa ndipo Ife tidzamva Mulungu bwino lomwe kudzera ku abale ndi alongo, ndi ngakhale kudzera mmalemba pamaene tiwerenga. Pamene ife tikhala mnjira ya Mulungu, ife timafewa. Kuwala kwa Mulungu kulowa. Mvula ya Mulungu ibwera ndi kumaliza kudzadza ife, ndi kuchotsa mphepo zoipa mwa ife. Pali chiyembekezo chambiri ngati ife tikhala mu njira ya Mulungu! Palibe chiyembekezo ngati ife sitikhalala mnjira ya Mulungu.

Ife tamanga munjira yolakwikwa kwa zaka zambiri. Mipingo yambiri kuzungulira padziko lapansi ili ngati chomera pansu padengu. Iwo akhza kumva ziphuzitso zabwino, koma iwo alibe kuwala kwambiri munyoyoyo yawo. Ambii ndi akufa, ena ndi okhinimbira. Ife tifunika kuchotsa dengi ili pachomera. Njira yaikulu yimodzi yochitira ichi ndi kulowerana mwa pamtima ndi wina ndi mnzake, kuthandizana ndi wina ndi mnzake, kulimbikitsana wina ndi mnzake, kukondana wina ndi ,mnzake tsiku lililonse.

Iye akumanga anthu a Mphamvu

Iye akumanga anthu kulamanda

Iwo akuyenda pamodzi ndi Mulungu

Ndipo iwo akukula ndi Dzina Lake Lopambana

Mangani Mpingo Wanu, Mbuye,

Tipangeni ife amodzi Mbuye,

Mu Ufumu wa Mwana wanu,

Mangani Mpingo Wanu Mbuye

Tipangeni ife amodzi, Mbuye,

Mu Ufumu wa Mwana Wanu.

Yendani Ulendo

Baibulo ndi loona mnjira iliyonse. Izi ndi zokhudza Yesu ndi omutsatira ake. Izi ndi nkhani za m'mene amawawidwira mtima ndi

mmene amaphunzirira kudzera mmakhalidwe awo ndi Mulungu. Ife tikhonza kuphunzira kuchokera munkhani zawo, koma tikhonzanso kuphunzira: pakukumana ndi kuonana ndi Mulungu pamodzi pamoyo wathu wa tsiku ndi tsiku. Mu ichi nafe tili “malembo amoyo.” Zolembedwa zonse mu dziko lapansi sizinganthe ife monga m'mene moyo wapamodzi ungatisinthire ife. Zinthu zakuya zomwe tizifuna sizidzafika pansa pa mitima yathu pamene zingawerengedwa kuchokera pa pepala chabe. Pamene tikonza zinthu pamodzi tsiku lirilonse, Yesu aliphunzitsa ife ziphunzitsa zakuya zamoyo zomwe sitingaziphunzire kuchokera m'Baibulo, “ngakhale zoonadi ndi eklezia—mpingo.” “MOYO umasanduka kuunika kwa anthu.”

Moyo siunapangidwe kukhala ngati sukulu ya galamala yomwe timakaphunzirako mfundo zina ndipo kenako kukhulupirira ndondomeko ina kapena zinthu. Malo mwake Mulungu watiyitana ife kukhala amuna ndi akazi a Mulungu chimodzimodzi monga omwe adaliko pasadabwere ife—olumikizidwa kwa Mulungu yemweyo amene iwo adalumikizana naye—okhala m'chikondi chozama monga iwo adaliri. Kuti chimene tichichite kapena kuchikwanitsa, ife tiyenera osati kudziwa momwe iwo amadziwa zokha. Koma tiyenera kumva chimene iwo amamvera, Mulungu ayenera kuti—tenga paulendo onga ngati wawo. Tsono ife titenga ulendo umenewu mukugwiritsa ntchito Mau a Mulungu kumodzi ndi moyo wathu. Ife tiyenda ulendowu ndi misozi m'maso mwathu, ndikuthandizana wina ndi mnzake—mu nthawi yoipa ndi nthawi yabwino—ndi maso athu pa chiyembekezo chathu, Messiah wathu. Ife tikupita chitsogolo, kukhulupilira kuti Mulungu akhala otipatsa wathu, kutithandiza pomwe tikhala pamodzi.

Petro adakana Yesu atayenda ndi Iye kwa zaka zitanu, koma pamene iye adamva tambala atalira, zidamuswa mtima wake. Ndipo pomwepo iye adabwererapamodzi ndi mbale wake Yohane. Ichi ndi chimodzimodzi ndi ife. Pali nthawi imene ife tidzapanga zinthu zoipa ndi nthawi pamene ife tidzapanga zinthu zabwino. Koma chili chonse tipange, ife tiyenera kupangira pamodzi ndi maso athu pamodzi ndi Yesu ndi kulola Iye atipange ife akuya mukudalira pa Iye pamene masiku akupita. Moyoudakhala luwala kwa anthu.” Ife tiyenera kuphunzira kwambiri zakhudza Yesu kudzera mukukhala pamodzi ndi kuthandizana wina ndi mnzake- Mulungu, tithandizeni kutsegula maso athu.

Kudzodza Kwa Wonse Yesu Ndiye Banja

Mzuzu, Malawi Afirika 1996

Kuti ukathe kuyankhula mawu a Mulungu munthu uyenera kudzodzedwa. Kodi izi ndizo inu nonsenu mumaganizira maganizo anu? Ndili ndi uthenga wabwino wochokela kwa Yesu kunza kwa inu okhudza za zimenezi. Izi zikulankhuliridwa kuchokela kwa buku la Yohane woyamba chapter 2 (okhululupira) kuti muli nako kunzodza pa inu koono osati kwachinyengo. Mzimu wa Mulungu, Yesu amene anali mphunzitsi wamkulu akhala mwa inu. Yesu ndi mphunzitsi wamkulu, wodabwitsa komanso wamphungu. Paulo adanena kuti ngati mulibe mzimu wa Yesu mwa inu ndiye kuti simuli aiye. Ngati inu muli mkhristu, ndiye kuti Yesu khristu adali munthu odzodzedwa kuposa munthu wina ali yense adakhalapo-Iyeyo akhala mwa inu. Uku ndiko kunena kuti ngati muli Mkhristu, ndinu wodzodzedwa. Alleluya!

Osakhala ndi udindo kapena dzina – Koma ntchito yochita.

Pali nthawi zina pakati pa anthu okhulupirira pamapezeka ntchito yoyenera kuchita. Pamakhala ntchito ngati kusamalira ana, kugawa chakudwa, kusamalira chuma, kusamalira amai amasiye komanso ana amasiye, kuthandiza kusamalira zinthu kapenanso nyumba za anthu, kukonza mapaipe odutsira madzi a zimbudzi, kuikira magesi, kusoka zovala kapenanso kunthandizana kulima munda. Pali ntchito zambiri muthupi la Yesu. M'buku la Machitidwe makamaka mutu wa 6 padali ntchito yoyenera kuchitidwa. Mchitidwe amu (malembo) m'mawu a mulungu sizimanena “zokhudza kudzodza kokhala m'busa yekha ayi.” Anthu asanu ndi awiri omwe akufotokozedwa mukhaniyi adali anthu wamba chabe amene adadzadzidwa ndi mphamvu ya mzimu woyera komanso nzeru. Iwo chikhalilecho adali (akutumikira) akugwira ntchito yabwino ya Yesu.

Adali ndi mbiri yabwino yokhudza khalidwe lawo lodzichepesa ngati atumiki a Yesu. Koma padali ntchito yofunika kudyetisa amai amasiye. Ndi chifukwa chake mubuku la Machitidwe mutu 6 likufotokoza za kuika kwa manja osati ngati kupemphera kwa Yesu koma kugwira ntchito.

Monga molingana ndi Baibulo anthuwa sadali madikoni ngati mmene tingaganizire ambiri aife. Monga mmene iwo adalili adali oposa udikoni. Timamva tikawerenga mbuku loyamba la Timoteyo mutu wachitatu (3) timawerenga kuti dikoni ayenera kukhala mwamuna (wokwatira) wapabanja, koma monga mmene tikudziwira bwino ife tonse, anthu awa sadali okwatira kapena adali ndi ana ayi.

Tikumva nkhani inayake mmbuyomo, Paulo adapita kukaona Filipino, amene adali mmodzi wa madikoni asanu ndi awiri. Kodi mukukumbukila kuti Filipino adali ndi ana a kazi anai amene nawo amene adachitapo ulosi? Mzimu woyera umafotokoza bwino lomwe za Filipino ngati “m’modzi mwa anthu asanu ndi awiri,” osati “modzi wa madikoni asanu ndi awiri.” Kudali madikoni ambiri m’mpingo yochuluka ya m’nthawi imeneyo koma mzimu woyera siukutiiza kuti, Filipino, adali m’modzi wa madikoni asanu ndi modzi.” Koma mzimu woyera ukutiiza kuti Filipino m’modzi wa anthu asanu ndi awiri. Iyi ndi fundo yofunika kwambiri. Pali kusiyana pakati pa Dikoni ndi munthu wina amene adasankhidwa ku utumiki.

Dikoni amakhala ndi ntchito yopitilira, Koma anthu asanu ndi awiri omwe adasankhidwa mabuku la Machitidwe Atumwi mutu wa chisasnu ndi chimodzi (6) tikumva kuti adasankhidwa ku utumiki wapadera. Ndipo tonse tikuntha kuona kuti ntchito ya utumiki wawo idasintha pomwe zinthu zidayamba kusintha mu Yelusalemu. Filipino adapita ku Samaliya, Stefano adanka naralikira masunagogi kumene tikumva kuti adaponyedwa miyala naphedwa koma sitikumvanso kuti iwo adapitiriza kupereka chakudya kwa akazi amasiye. Nthawi zina timayenera kuyika manja pa anthu okhulupirira kuti Mulungu awatume ku ntchito yapaderadera, koma ngati ntchitoyo yomwe adasankhidwira yatha sapitirizanso kukhala maudindo omwe kalero adasankhidwira. Pano pali mbali yosiyana, ngakhale, thawi zina pamene Mpingo wakula kwambiri, kuti ukhale ndi madikoni ndi akulu a Mpingo. Izi zimangokhala ntchito zopitiriza-pitiriza imene imalira zinthu zambiri monga mwa udindo kuti ukathe kuthandiza munjira zambiri.

Pamene mudzatchedwa mkhristu, Yesu adzakusanjikani manja ndipo pomwepo mudzakhala wansemble. Mudzakhala olankhula koma okonda mawu a Mulungu. Pamene mpingo ukukula komanso kusintha, pamakhala ntchito yoyenera kuichita kapena kuti mpingo umasankha mwa anthu ake amene alipo ena monga awiri kapena anai amene ali odzala ndi Mzimu woyera ndi nzeru. Kapenso ngati ntchitoyo ioneka kuti ndiyaikulu amasankhirapo anthu ena asanu ndi awiri wodzala ndi mzimu woyera ndi nzeru kudzaika manja pa iwo pamodzi komanso kuwasankha iwo ku utumiki. Koma izi zimakhala choncho ngati pokhapokha pali ntchito apo bi ayi, anthuwo amakhaladi okhulupirika ndi omvera ku ntchitoyo ndipo adzakhaladi ndi udindowo, koma ngati kudzaoneka kuti sali okhulupirika pa udindowo, udindowo udzachotsedwa kwa iwo. Koma ngati alibe okhulupirika adzagwira ntchito paudindowo kufikira ntchito yomwe adasankhidwira yachitika. Pamene tikamanena za Madikoni ndi Akulu a Mpingo, iyi simakhalanso ntchito. Komanso ndi zoonza kuti mwina nthawi zina zimatha kutheka kuti ngati akhala anthu osakhulupirika amatha kuwachotsa pa udindo wawonso.

Mphatso ya Mtumwi

Mtumwi Paulo adanena kuti iye ndi kapolo wosankhidwa ndi Mulungu. Sichinali kuti adali munthu wapaderadera ayinso, koma kuti Mulungu adali kufuna kuonetsera chifundo chake. Izi zidali chomwecho ndi atumwi onse. Iwo sadasankhidwe chifukwa adali anthu apaderadera ayi. Iwo adasankhidwa pa mpikisano wa chifundo cha Mulungu. Paulo adanena zimenezi kwa akhristu aku Mpingo wa ku Korinto kuti ngati sangachite ntchito yomwe Mulungu adamuitanira ndiye kuti chinthu china chake chikhodza kuchitika monga ngati matembelero. Paulo adanena kuti udindo wa mphatso ya utumwi ndiwo nthawi zonse ayenera kukhala munthu wokhulupirika ngati kapolo kuti ukathe kuwauza anthu ena za ukulu wa ulemerero wa Yesu. Choncho adakhala kapolo wa uthenga wabwino wa Yesu, ndipo m’malo mwake adapereka moyo wake pa mtengo uli wonse omwe akadayenera kupereka, kuti akathe kukwanitsa kuwauza anthu ena za uthenga wabwino wa Yesu.

Pali mphatso zambiri muthupi la Yesu khristu ndipo mphatso iliyonse ili ndi kufunikira kwake. Paulo adanena kuti mphatso zomwe aliyense

adali nazo zinali zofunikira mwapadera, kuti aliyense athe kutumikira ngati wansembe kuti akathe kuwauza anthu ena za Yesu Khristu. Iye adanenanso kuti anthu ena omwe amanena za Yesu adzalandira mphoto. Koma mtumwi Paulo adanena kuti, ali otemberereka ngati sangawauze anthu ena zokhudza Yesu. Mphatso ya utumwi ndi ubwino wake ndi umodzi komanso yapaderadera komanso yosowa kwambiri. Komanso ili ndi zopereka mtengo wache zambiri, monga kulankhula kwa Paulo. Atumwi ali ngati mizati m'nyumba ya Yehova. M' buku la Aefeso mutu 3, Paulo akulankhula za zinthu ziwiri zomwe iye amayenera kuchita pa udindo wake ngati mtumwi. Adanena chinthu chimodzi pa (versi la 8) ndiko kuuza anthu ena za chuma ulemerero wa Yesu. Mundime la a Paulo akunena za chinthu chachiwiri chimene iye adaitanidwira, ndiko kuti akathe kuwafotokozerana anthu momveka bwino m'mene angakhalire mu ulemerero odabwitsa wa Yesu Khristu. Iye adanena kuti adzawaphunzitsa m'mene angakhalire ndi moyo wodabwitsa wa Yesu komanso m'mene angasanthulire moyo wodabwitsawu wa Yesu m'moyo wawo.

Mubuku loyamba la ku Akorinto mutu wa 3, Paulo akudzitcha yekha womanga waluntha. Iye sadanene chinthuchi chifukwa adali onyada koma Mulungu adachiika chinthuchi m'mafupa ache. Mulungu adampatsa iye chifundo komanso kumkomera mtima pomupatula iye mwapadera kuti akhale nayo mphamvu yotha kuona zinthu zimene ena samakwanitsa kuona. Mu buku la Akorinto loyamba mutu wa 15: ndime ya 10, Paulo adanena kuti iye adali chigawenga koma Mulungu sadamukhulukire kokha koma adamupatsa mphatso yapadera. Yesu amapereka mphatso zambiri, zosiyanasiyana. Muzinthu zonse zomwe Yesu adali ziwalo zake zonse, adazipereka ku Thupi lake. Mukunena kwa tchutchutchu mphatso zonsezi ndi zofanana chifukwa zonsezi ndiye Yesuyo. Koma mphatso yomwe Mulungu adamupatsa Paulo idali ya utumwi. Paulo adanena kuti iye “sadali munthu oyenera kukhulukidwa machimo ake. Koma chifukwa adamukhulukira machismo ake ndikumupatsa mphatso, iye adzagwira ntchito modzipereka kwambiri ngati njira imodzi yonenera zikomo Inu Mbuye Yesu pondikhulukira machimo anga.” Mphatso imeneyi idali kuti akathe kuwafotokozerana anthu ena za chuma cha mtengo wache wapatali cha Yesu.

Chifukwa kuti Paulo adali ndi mphatso yamtengo wapatali yoona zinthu zomwe anzake sankazona, iye adafunitsitsa kuthandiza anthu onse a

Mulungu kuti athe kuona m'mene angayendere pamodzi. Umu ndi m'mene mphato ya utumwi ilili, n'chifukwa chake mphatso imeneyi ili yofunika kwabasi mumpingo pa dziko lonse loti zungulira. Tayerekazani mutayika akhristu odzipereka okwana zanalimodzi pamalo amodzi, onsewo adzakonda Yesu ndi mitima yawo ndipo kudzakhala kufuna kwawo kuti amumvere Yesu. Koma kopanda chiyanjano ndi mtumwi nthawi zina zimakhala zovuta kudziwa m'mene angayendere pamodzi. Angadziperekere, akhristu okondana angamavulazane wina ndi mnzake, koma mphatso yomwe Yesu amapereka kwa iwo ya utumwi imawathandiza kuti agwire ntchito limodzi.

Kuika Ziwalo Zonse Pamodzi

Tikhoza kutenga ziwalo zonse za galimoto – chowongolero, bampala, mota, chitseko – ndikuziunjika munyumba imodzi. Zonsezo zikhozao kukhala ziwalo zodabwitsa, koma m'malo mwake simungathe kuyendetsa mtunda wautali ngati zidutswa zonse za galimoto sizinaikidwe pamodzi. Zoonadi zeni zeni pa nkhaniyi ndi yakuti mukhoza kupita kuli konse ndi galimoto imeneyi. Mphatso ya utumwi ndiyo imasonkhanitsa mphatso zonse pamodzi. Mumpingo tikufuna mphatso yomwe ingapangitse kuti zidutswa za galimoto zikhale pamodzi. Izi ndi zimene Paulo amanena pa buku la Aefeso 3. Iye amawauza anthu za ukulu wa dzina la Yesu limene limathandiza kuika mpingo pamodzi. Paulo adafuna kuika mpingo pamodzi kuti itchedwe nyumba ya Mulungu. Mphatso zonse komanso akhristu onse odzipereka amafuna mphatso ya utumwi kuti iwathandize kuika nyumba pamodzi.

Mubuku la Aefeso mutu 4, Paulo adanena kuti Mulungu amapereka mphatso kwa mpingo – mtumwi, mneneri ndi mphatso zina kuti pamenepo tikakule tonse pamodzi. Imatiphunzitsa kuti tisakhalenso makanda, imatithandiza kuti tikule kufikira muuphumpu wonse wa Yesu Khristu, kutithandizira kuti tikaumbike pamodzi. Paulo adanena za kufunikira kwa mphatso ku mpingo kuthandizira anthu abwino kuti amangirirane pamodzi.

Makalata ambiri a Paulo amalankhula za ntchito zochitika zenizeni. Iye sadakambe zambiri za Yesu Khristu, koma makamaka zinalimbikitsa okhulupirira m'mene angakhalire pamodzi kwa wina ndi mzake. Iye

adawaphunzitsa iwo ndi zinthu zochitika zeni zeni kuyambira ndalama, ukwati, ana ndi akazi amasiye, komanso m'mene angamangirirane mumpingo mokhudzana ndi ulamuliro. Iye adawaphunzitsa zokhudzana ndi kupembedza kwawo pamodzi, misonkhano, komanso m'mene angamangirirane pa zinthu zosowa zawo wina ndi mnzake.

Chiphunzitso cha zidutswa zabwino za galimoto (kuti m'mene zikhalire galimoto) izi ndi zimene mtumwi Paulo amachita ndi mphatso yache iye amafuna kuwaphunzitsa kuti akhale pamodzi ndi kupita kwina kwake, ifeyo sitikufuna kukhala ngati mkoko wanthochi omwe siungathe kupita kwina kuli konse. Iye tikufuna kukhala Basi ya Yesu yomwe ingakwanitse kupita kwina kulikonse. Tikufunika kumangika pamodzi kenako ndi kuphinzira m'mene tingawirire ntchito muchikondi.

Paulo akutiuzwa kuti ndichinthu chabwino kukhala ndi mafunso a zinthu zochitika. Mubuku la Akorinto woyamba mutu 1, tikuwerenga za banja la Kloe lidayenda mtunda wokwana 100 milosi kuti akathe kumufunsa mafunso Paulo. Amakamufunsa za magawano chomwe iwo mu mpingo wakumeneko zokhudzana ndi mabanja, komanso chomwe iwo angachite tchimo likakhala liri pakati pawo. Chifukwa kuti mphatso yake idali ya utumwi adatha kuona chomwe iye angachite. Anthu a Mulungu adali kumufuna Paulo kuti athe kuona komanso kuwathandiza. Paulo chonsecho sadali “opsa wina aliyense ayi.” Iye adali kudziwa bwino lomwe za chifoko chake mumtima mwake, kuti tsiku lina iyenso adachitapo uchimo asadatembenuke. Koma chifukwa Mulungu adamukonda Paulo, n'chifukwa amafuna kunena “kuti zikomo” pogwiritsa ntchito mphatso yake kwa anthu a Mulungu.

Mafunso Ofunsa Zinthu Zenizeni

Zokhudzana Ndi Udindo Wa Amuna Ndi Akazi

Komanso ndikadakonda amai adzivala bwino modzilemekeza, osati ndi tsitsi langale zamtengo wapatali ngati golide, kapena zovala zamtengo wapatali, akhale ndi makhalidwe abwino ovomere kwa akazi onse wopembedza Mulungu. Akazi ayenera kuphunzira mwakachetechete, koma sindilola ine akazi ayenera adzimveke okha ndi chovala choyenera, ndi manyanzi, ndi chidziletso, osati ndi tsitsi loluka, ndi golide kapena

ngale, kapena Malaya a mtengo wache wapatali, komatu; (umo mokomera akazi akuvomereza kulemekeza Mulungu), mwa ntchito zabwino. Mkazi aphunzire akhale wachete m'kumvera konse. Koma sindilola ine kuti mkazi aphunzitse, kapena kulamulira mwamuna; komatu akhale chete. Adamu adali oyamba kulengedwa, pambuyo pake Eva. Adamu sindiye adayamba kunyengedwa ndi chinjoka koma mkazi ndiyo. Mkazi adapulumutsidwa mwakubala mwana ngati akhala n'chikhulupiriro, n'chikondi ndi n'chiyeretso. (1 Tim 2:9-15)

Izi zikungofanana ndi mawu omwe akupezeka m'buku loyamba la 1 Akorinto mutu 14, Paulo adalemba mawu onsewa ndi mzimu wa Mulungu. Ndiye n'chifukwa ndikufuna kuti timvetsere zomwe mzimu woyera amaganiza komanso pamene iye amalemba zinthuzi. Mzimu woyera ndi munhu amakhala ndi maganizo komanso zokhumba, monganso mene inu ndi ine tili. Inuyo mukalankhula kanthu kwa ine ndiye kuti mukulingalira zinthunzo komanso muli ndi chikhumbitso chachikulu kuposa umo mwalankhulira. N'chifukwa chake ndafuna kuti timvetsere zimene mzimu woyera amamvera komanso kulingalira chifukwa mzimu woyera ndi munthu, osati mawu okha ayi.

Mtima wake wa Mzimu Oyera umakonda mai kapena bamboo chimodzimidzi. M'bukhu la Agalatiya mutu 3, iye amanena kuti palibe mwamuna kapena mkazi tonse ndife amodzi mwa khristu. Palibe M'yuda kaya M'heleni, palibe mkazi, palibe mwamuna, palibe wakuda, kapena woyera, kapena wachikasu. Alleluya!! Koma tsopano tonse ndife a Yesu. Kodi Yesu adali ndi maonekedwe anji? Ndani akuchidziwa chinthuchi? Iye ndiye wodabwitsa! Chifukwa cha chimenechi, ndichifukwa chake tilinacho chikhulupirio mwa Yesu Khristu, tonse timavala Yesu, palibenso Myuda kapena M'heleni, kapolo kapena mfulu, mwamuna kapena mkazi. Izinsu Mzimu Oyera adalankhula mubuku la Agalatiya mutu 3.

Malingaliro A Mtengo Wapatali Okhudza Za Ulamuliro

Pali zinthu zambiri zomwe Mzimu Oyera amaganiza zokhudzana ndi mkazi kapenanso mwamuna; zinthu zimenezi ndi zamtengo wapatali tiyenera kuzimvetsa pamodzi. Pamene tikulingalira za mwamuna kapena

mkazi, tikuona kuti Atate ndi mutu wa Khristu. Khristu ndi mutu wa mwamuna. Mwamuna ndiye mutu wa mkazi. Kodi Yesu sindiyenso mutu chimodzimodzi Atate wake? Yesu adanena, “Ine ndi Atate ndife amodzi.” Koma Atate ndiye wamkulu kuposa khristu, ngakhale ndiwo amodzi. Tomasi adanena ndi Yesu, “Ambuye wanga ndi Mulungu wanga.” Atate ndi mwana ndiwo amodzi.

Chachidziwikire kuti Yesu ndiye mutu wa mwamuna. Koma ngati tidavekedwa Yesu tili naye pamodzi Yesuyo. Apa tikuona kuti pali ulamuliro pakati pa mwamuna ndi mkazi. Mwamuna aposa mkazi chimodzimodzi Yesu ali oposa mwamuna. Pamene mwamuna ndi mkazi ndiwo amodzi mwa khristu. Choncho, kunena momveka bwino tikutathauza kuti mwamuna ndi mkazi ndiwo amodzi (ofanana). Koma ngakhale zili choncho pali ulamuliro pakati pa mwamuna ndi mkazi.

Zinthu izi ndizo za mtengo wapatali ndipo muyenera kutchereza. Mwamuna angathe kutumikira mkazi ndi mtima wanu wonse. Mwamuna ayenera kukonda mkazi kumuchengetera mozama. Mwamuna, munjira ina iliyonse ayenera kukhala kapolo kwa mkazi. Ngati chimodzimodzinso khristu adabwera kudzatumikira mpingo. Ngakhale kuti Yesu angathe kusambitsa mapazi athu ngati kapolo angachitire, komabe ali ndi ulamuliro. Chimodzimodzinso, mwamuna achengetere komanso akonde mkazi, mpakana adadziyesera yekha kapolo kwa iye munjira ina iliyonse, iye ali nawo ulamuliro pa mkazi, ndipo mkaziyo ayenera kumvera ku zimenezi.

Ngakhale kuti zili Yesu ali ndi okoma mtima kwa ife komanso kutikonda ife sindicho chifukwa kuti ife tiyiwale ulamuliro wake, kodi sichoncho? Muli dongosolo mwa Mulungu la kachitidwe kazinthu. Muli ulamuliro mwa Mulungu. Pamene Mzimu Oyera amalankhula nafe pa 1 Akorinto mutu wa 14, ndiso 1 Timoteo mutu wa 2, izi sizikutanthauza kuti amuna ndi olamulira, kulamulira mkazi ndi nkhonya ya chitsulo. Komanso mkazinsu sikapolo kuti ayenera kuti adzithawira kukonda mumtima. Tiyenera tikondwerere mphatso adapereka kwa akazi athu, ngakhalebe amadzipereka pa mphatso zomwe Mulungu adawapatsa mitima mwawo. Koma akazi ayenerabe kuzindikira za ulamuliro umene Mulungu adauyika pa amuna. Choncho zinthu zonse ndi zamumtima. Zinthu zonse zotchedwa chi khristu zimakhudza mtima osati malamulo. Yesu sadatininkhe ife malamulo m'malo mwake adatipatsa ife mtima wake. Iye

adatiphunzitsa ife kuganiza munga momwe iye angaganizire. Choncho cholinga chatu chachikulu ndicho kukhala ndi mtima omwe iye amafuna ife titakhalira munga mawu opezeka mabuku a 1 Akorinto 14, kudzanso 1 Timoteo 2, Baibulo sindiyo Buku la malamulo lokha komanso m'mene timapezamo moyo. Kodi zimenezi zikuoneka bwanji m'moyo wathu wa tsiku ndi tsiku? Muchiyanjano chomwe chilipo pakati pa mwamuna ndi mkazi, mwamuna adzadyetsa, kusamalira, komanso adzachengeta mkazi wake. Adzautaya moyo chifukwa cha mkazi munjira ina iliyonse, ngakhale kupitirira apo kukhala kapolo chifukwa cha Mpingo. Chimodzimodzi mkazi ayenera kukhala otchereza kwa mwamuna chifukwa ndi mtima wake. Mtima wake wa mkazi ndi kutchereza mawu onse komanso kuchita zomwe mwamuna akufuna. Ili si lamulo koma m'mene Yesu amakondera kuti ife tizikhalira m'mtima mwathu. Mukuchulukira komwe mwamuna angakhale nayo nthawi yochita zomwe tatchula pamwambapa, mochulukira mwamuna adzamvera kulankhula kwa Mulungu. Komanso mkazi akakhala ndi moyo womvera kwa mwamuna, iyenso adzakhoza kumvera kulankhula kwa Mulungu. Mawu amanena kuti, “*Anthu awiri adzayenda bwanji asanapanganiretu?*”

Ulamuliro Umatimasula Ife!

Zinthu zonsezi tatchulazi, ndi zofunika. Ngati mpingo uli pamodzi, komanso ngati mitima yathu ndi maganizo zili zabwino, ndipo mwamuna adzakhala wochita ulemu komanso okonda akazi onse (am'mene sadzasowa ngati mipando). Amuna adzayamba kukonda mphatso zomwe zili mwa mai ndipo iwo sadzalola kuti mphatso zomwe zili mwa iwo zikwiririke m'nthaka. Nawonso alongo adzayamba kulemekeza abale, pamene ali pachiyanjano cha oyera mtima, ndipo iwo ngati akazi adzatha kudziwa ulamuliro wa amuna osafuna kukhala pamwamba pa ulamuliro wa amuna. Paulo adanena, “Ine sindilola mkazi aphunzitse komanso akhale ndi ulamuliro pa mwamuna.” Ngakhale angathe kupereka mphatso zawo. Mwachitsanzo: Ngati mlongo wina ali ndi kanthu kena m'mtima mwake kofunika kulankhula, iye sayenera akwirire luntha lake. Iye sayenera kuti akwirire mphatso yomwe Mulungu adamupatsa mphatso yomwe ili mwa iye. Ife timafuna zonse za Yesu. Choncho ngati mlongo ali ndi kanthu komwe kakumutentha mumtima mwake kofunika

kulankhulidwa, wayenera mlongoyu apemphe abale pofuna kulemekeza ulamuliro oposa wake nthawi zonse. Ngati pali mwamuna wa ulamuliro oposa wake, ayenera kumufunsa ngati koyenera kulankhula. Komanso ngati kungakhale kotheka mwamunayo angathe kufunsa mpingo ngati kuli koyenera kuti mlongoyu alankhule kapena ayi. Ngati kungakhale kuti mwamunayo aona kuti ndi kosavomereza mlongoyu kulankhula komanso mpingo wawona kuti mkaziyo asalankhule panthawiyo, iye ayenera akhale okondwa kukhala chete. Mkaziyo sayenera kuti akwiye chifukwa adakanizidwa kulankhula. Sayenera kunena taonani, “kuyambira lero sindidzalankhulanso kanthu pakati pa mpingo.”

Umu ndi m'mene amai angakhalire a Yesu kwa aliyense, komanso mwamuna pokhalabe ndi ulamuliro. Wamuna angathe kutenga mphatsoyo, koma munthu wa mkazi samadziika yekha pamwamba pa mwamuna. Pamene muwerenga ziphunzitso za mawu a Mulungu nonse pamodzi, chimene mungaone ndi chakuti Mulungu ali mtima wolunjika kwa amai. Mkazi sindiye mpando kapena gome m'chipinda. Mlongoyu ali ndi moyo mwa Yesu ndipo tiyenera kukhala omufunitsits mlongoyu. Komanso mlongoyu ayenera kumvetsetsa za ulamuliro wa Mulungu ndipo sayenera kukhala onyada. Iye ayenera kukhala odzichepetsa kuti athe kudzipereka yekha nsembe. Iyi ndi dongosolo la Angelo, dongosolo la Mulungu Atate ndi dongosolo la Yesu mwana, komanso dongosolo la mwamuna ndi mkazi. Tonse ndife amodzi, koma pali ndondomeko mwa Mulungu imene imathandiza kuti zinthu ziziyenda bwino. Ndife ofanana, komanso mphatso ya mkazi ikhoza kukhala yabwino koposa poyerekeza ndi ya mwamuna wake, koma Mulungu adamupanga kukhala wa mwamuna. Ichi n'chifukwa chake pali dongosolo. Komanso mwina iye samayenera kukhala ndi ulamuliro. Koma Mulungu amasankha zinthu zimene tiyenera kuzilemekeza, choncho tonse pamodzi tiyenera kugwira ntchito yobweretsa mphatso komanso kukonda ndondomeko yomwe Mulungu waika kuti tiyende pamodzi tonse.

Kumene ndimakhala ine kuli amai ambiri omwe ali ndi mphatso. Mpingo kumeneko ndi odalitsika kwambiri chifukwa uli ndi amai olimba kwambiri mwa Yesu. Iwonso akhoza kukuuzza za ndondomeko yomweyi monga ngati chinthu choyendetsa zinthu mwa dongosolo la Mulungu – chinthu ichi sichiwakanikiza iwo pansu; koma m'malo mwake chimawamasula. Pali

ufulu wambiri popeleka mphatso zawo ngati nsembe m'malo mongotenga potsatira ulamuliro. Ndi chinthu chamtengo wapatali kukhala munthu wodzipereka. Akazi pa iwo okha adzakhoza kukuuzani kuti ulamuliro umawamasula m'mitima yawo ndinso umawapanga iwo kuyimba nyimbo m'kati mwawo pamene akupereka nsembe ya mphatso zawo koposa kutsatira ndondomeko. Choncho pamene sitiri kufuna kupondereza pansu mphatso zonse, mphatsozo zimabwera ngati zopereka kuchokera kwa alongo, izi ndi zoona makomo, komanso m'ziyanjano za oyeramtima. Uwu ndiwo mtima omwe Yesu amaufuna – mtima omwe iye angaudalitse.

Kodi mukukumbuka zomwe Ambuye Yesu adanena kwa Kentuliyo, Msirikari wa Chiroma? Iye adanena kwa Kentuliyoyo kuti mwa iye, adaonamo chikhulupiriro chachikulu kuposa anthu onse M'Israeli. Chikhulupiriro chomwe Yesu adali asanachionepo chidapezeka mwa munthu mwamuna amene amadziwa kukhala pansu pa ulamuliro komanso ndikukhala ndi ulamuliro. Mlonde wachiroma adanena kuti Iye angathe kunena kwa watchito wake “Pita”, ndi iye adzapita. Adzanenanso kwa waichito wina “Bwera kuno”, ndipo iye adzatero. Iye adanenso kuti ndiye munthu odziwa ulamuliro ndiko kunena kuti Pita ndinso Bwera ulamuliro wake. Yesu adanena kuiti uyu ndi munthu wachikhulupiriro Chachikulu yemwe Yesu adamuonapo chifukwa amadziwa kumvera ulamuliro. Ichi chinali chomwe chinamumasula iye, osati chomwe chingamukanikize iye pansu.

Pamene Yesu ali mutu wa Mwamuna, mwamuna amamasuka. Yesu adanena kuti ngati sitingathe kukhala kapolo wache tingathe kukhala kapolo wa tchimo. Ngati sitingathe kumulola Yesu kukhala Mbuye wathu, uchimo udzakhala mbuye wathu. Koma ngati mwana adzatiyesa ife mfulu tidzakhala mfulu ndithu. Kodi mukutha kuona zinthu izi m'moyo mwanu? Mukangomumvera Yesu, inuyo mudzamasulidwa? Koma pamene mungakhale osamvera Yesu ndi osalungama m'mtima mwanu.

Izi ndi m'mene zilili ndi mwamuna ndi mkazi. Iye tikatsalira ulamuliro wa Mulungu, sitikhalanso akapolo; ndiye mfulu. Koma ngati sititsalira timakhala akapolo ku zolakwika zathu. Mkazi yemwe Sali pansu pa ulamuliro ndiye osalungama m'mtima mwake. Iye adzakhala okhumudwa ndi osakonzeka, Mulungu ndiye amapereka ulamuliro m'banja komanso m'mpingo – izi sizitanthauza kuti pali munthu wina yemwe ali wabwino kwambiri kuposa

wina ayi, kapena kuwafotokozero anzakenso kuti achite chiyani powalamulira chomwe angachite. Iye amapereka ndondomeko ndi ulamuliro kuti tonse tikhale omasuka kuchikondi ndi dongosolo la Mulungu.

Kulankhula Ndi Atate Ngati Banja

Chomwe tikufuna kulankhula apa ndi m'mene tingakhalire, osati m'mene tingakhalire ndi Chiyanjano. Kuyankha mafunso amoyo watsiku ndi tsiku ndikophweka poyerekeza m'mene zingaonekere pachiyambi. Pamene tidzathe kukhala ngati banja muchoonadi pomwepo zithu zidzayamba kumveka bwino. Anthu ambiri ali okodwa pakati pa banja ndi chipembedzo ngati kabungwe. Gulu lina la anthu achabe a chipembedzo ndi banja. Pamene enanso akodwa pakati pongokhala opita kutchalitchi ndinso banja. Pamene chonsecho Mulungu akubweretsa Mpingo wake kuti ukhale ngati banja, pamenepo zinthu zimayamba kumveka bwino. Pamene tidzadziona pa ife tokha ngati banja, mayankho a mafunso ambiri omwe tingakhale nawo amayamba kupezeka. Chifukwa timayamba kukondana wina ndi mnzake mowirikiza, timagawana mbali ina iliyonse ya moyo wathu umalukika pamodzi tsiku lili lonse, amuna amadziwa kukhala bwino ndi akazi komanso akazi nawo amadziwa m'mene angakhalire ndi amuna. Ngati tingadziwe m'mene tingachitire m'makomo athu ndinso makwalala, tidzadziwa m'mene tingachitire misonkhano.

Mu zinthu zonse, tiyenera kuzindikira ndondomeko ya Mulungu, komanso tiyenera kusauzima Mzima. Tiyenera kuzindikira dongosolo, komanso sitienera kukwirira luntha lathu. Choncho, ngati Oyera mtima asonkhana pamodzi Mulungu amapereka pemphero mumtima wanga, ngati munthu wamwamuna ndine oyeneranso kufunsa ngati kuli koyenera kuti ndipemphere. Koma ngati amene akufuna kupemphera ndi wamkazi ndi chichidziwikire kuti ayenera apemphe kaye mwamuna ngati kuli koyenera kuti apemphere, mwamunayo naye ayenera afunse anthu onse osonkhanawo, “Kodi ndikoyenera ngati mlongoyo ayenera kupemphera?” Ngati mwamuna ndi msonkhano onse aganiza kuti ndikoyenera, mlongoyo ali pansu pa ulamuliro. Iye ndiwokutidwa ndi ulamuliro ngati timulola iye kutero, koma ngati iye angachite zinthuzi payekha, izi zidzakhala kunja kwa ulamuliro (dongosolo). Koma ngati ife

tonse tingamlole kuti apemphere mlongoyo ali pansu pa ulamuliro ndipo nthawi yomweyo zinthu zili bwino. Zinthu izi nthawi ndizoona.

Tiyenera kumvetsa zinthu zina zake zokhudza pemphero. Mawu oti ‘Pemphero’ amamveka ngati achipembedzo ku makutu athu. Pamene tikhala ngati banja, mnjira yomwe tingagwirire tchito limodzi zimapangitsa kuti zinthu ziyambe kumveka bwino pakusonkhana ife. Pamene tidzakhale oyandikira kwambiri ndi Mulungu, mapemphero athu adzayamba kumveka. Mudzipembedzo zonyenga nazonso, anthu amapemphera mapemphero. Mwa Yesu, m'chikhristu, timakhala ndi chiyanjano ndi Atate athu okonedwa. Choncho, kunena kuti “Mapemphero okumana pamodzi amatanthauza chiyani?” Kodi zimatanthauza chiyani tikamanena kuti kukhala ndi banja la Mulungu pamodzi? Kodi mukutha kuona kusiyana” Wina ndi wachipembedzo, ndipo wina ndi wachiyanjano.

Sitimanena kuti “mapemphero” koma m'malo mwake timanena kuti kulankhulana ndi Atate – m'mene mwana amalankhulana ndi atate ake. Kodi mwana angakonze msonkhano ndi atate ake, kodi angathe kulankhulana ndi atate ake chifukwa amawakonda iwo? Tangoganizirani tiyana tating'ono titasonkhana m'kachipinda adzayenera kukonza msonkhano kuti akambirane ndi atate awo? Kodi adzapanga msonkhano ofuna kukumana ndi bambo wawoyo. Iyi sidzakhala mapemphero okumana. Koma m'malo mwake idzakhala banja kukumana pamodzi ndi atate wawo.

Tsopano ndiganiza mwayamba kuona mapemphero aumodzi amagwirira ntchito. Siziyenda zinthuzi! Zimene timachita n'chakuti ngati m'bale akufuna kulankhulana ndi atate ngati iye atha kulankhula ine ndifuna ndilankhule nawo atatewo!” Umu ndi m'mene timapempherera pamodzi pagulu. Umu ndi m'mene timalankhulirana ndi Mulungu pamodzi, pamene Mulungu akutakasa mitima yathu. Mlongo wina akhoza kufunsa m'bale wina, “Kodi chikhoza kukhala choyenera kulankhula ndi atate tsopano?” Iyeyo ali mudongosolo chifukwa ali pansu pa m'baleyo yemwe ali ndi ulamuliro pa iye. Koma izi sizitanthauza kuti mlongoyo alibe ufulu akutha kulongosola za dongosolo loyenera. Umu ndi m'mene tingamachitire tikakhala ndi mapemphero, chiphunzitso, komanso tikamafuna kuyimba nyimbo, chifukwa tili ngati banja pamodzi ndi Atate wathu.

Tikufuna tichotseretu miyambo ya anthu ndi chipembedzo-pembedzo zichoke zituluke ndipo ife tingokhala ana wina ndi mnzake. Sitikufuna kukhala achipembedzo, anthu ojera ndi Maina ndi zikhulupiriro za miyambo ya anthu. Tikufuna tikhale ana okondedwa wina ndi mnzake, komanso ndi atate tsiku ndi tsiku. Kukumana kudzadzisamalira kokha chifukwa ife ngati ana komanso banja tingathe kukumana nthawi zonse. Timalankhula ndi adadi athu nthawi zonse. Timabweretsa chiphunzitso cha Yesu Khristu kwa wina ndi mnzake nthawi zonse. Ngati zingapangike kuti takumana pamodzi muchipinda chimodzi, zimakhala zinthu zamphamvu. Komanso izi sizitanthauza kuti zikhoza kukhala zosiyana mphindi makumi atatu zikatha.

Funso Lokhudza Amai

Funso ndi ili: M'baibulo mawu a Mulungu amanena kuti pamene tisonkhana Amuna ayenera akweze manja awo mwamba, koma akazi ayi. Kodi akazinsoko akhoza kukwezanso manja awo mwamba? Kodi Izi zikhoza kukhala zabwino?

Funso Labwino: 1 Timoteo 2:8-9 akunena kuti “ndikufuna amuna onse kulikonse akweze manja awo kumwamba akamapemphera, popanda mkwiyo kapena kukangana kwina. Komanso ndikufuna amai adzivala modzilemekeza, ndi moyenerera osati ndi tsitsi loluka kapena dzovala za pa mwamba.

Paulo sakutanthauza kuti, amai sayenera kukweza manja awo mwamba popemphera.” Komanso sakutanthauza kuti abambo sakuyenera kuvala moyenera. Ngati m'bale angakwanitse kukweza manja, ayenera akweze manja ojera. Mawu akulu pamenepa ndi “kuyera.” Ayenera kukweza manja omwe ali odzipereka kutchito ya Mulungu komanso ofunitsitsa kumutumikira pokhapokha amai akagwiritsa udyo ulamuliro, koma ali ndi manja ofunikira motumikira Mulungu, iye wayenera kukweza manja ake mwamba. Mulungu sakutiiza kuti abambo sayenera kuvala modziyenereza komanso sakutiiza kuti iwo siyenera kukweza manja awo mwamba popemphera; kapena kuti ndi zabwino, ngati iwo ali ndi manja ojera, m'mene zilili zovomerezeka kwa amuna onse kuvala modzilemekeza.

Ubatizo Wa Yesu

September, 1996 Mzuzu Malawi

Kuzindikira Ubatizo

Zimene Mulungu anaika kukhala chinthu cha bwino monga mpatso chakhala chinthu chochitira nkhonkho. Monga thupi la Kristu likamakula monga ofanana ndi Yesu ndi zina. Tiyenera kudziwa kumasulira kwa kuti ubatizo ndi chiyani? Timaona mu chipangano cha tsopano mmene Yohane Mbatizi anabwera kudzawabatiza anthu kuti machimo awo akhululukidwe. Panalibe malemba mu chipangano chatsopano zoti Yohane adzabatiza anthu. Pamene Yohane anabwera anabviika anthu mu mtsinje wa Yorodani zinali zodzawitsa kwa anthu. Chifukwa panalibe uneneri wa ubatizo ndipo panalibe wina kale amene amadziwa mpaka Yohane anabwera.

Choncho kunali kosabvuta kuti Yohane ali kulakwa chifukwa panalibe pamene Baibulo limanena kuti ndibatizidwe mu chipangano chatsopano? Koma chifukwa Yohane anali bwenzi wa Mulungu ndipo anatumidwa ndi Mulungu ndi uthenga wabwino kwa anthu anabweletsanso ubatizo kwa iwo, ndipo amabwera kuchokera kumadera ndi m'midzi kuti kudzabatizidwa. Anthu ena amumpingo mu nthawi ya Yohane anati sitifuna ubatizo utiuze kuchokera mu ubatizo. Yohane kuti tibatizidwe Yohane sanathe kuwauza kuchokera mu Baibulo chifukwa munalibe chiphunzitso mu chipangano chakale. Koma Yohane anamvetsera kwa Mulungu ndi kumva mau a Mulungu za ubatizo. Anthu ambiri ndi Afarisi anati. Ai ubatizo Baibulo limanena momveka bwino kuti anakana chifuniro cha Mulungu ku miyoyo yawo pokana ubatizo ndibwelezanso kuti mumvetse bwino Baibuli limati anthu amene anakana chifuniro cha Mulungu mu miyoyo yawo.

Mwina sitidziwa bwino ubatizo mwina kunyowa konseko sitidziwa kuti ndi chiani kwa ife. Mwina sitingadziwe za izi koma ndi zofunika kwa Mulungu mum moyo wathu. Mwina sitingadziwe kuti izi ndi chiani. Oma ndi zofunika kwa Mulungu ndiye ndizo funikanso kwa ifenso.

Kufunika Kwa Ubatizo Kwa Yesu

Mukuyangana mu chipangano chatsopano ndi chiphunzitso cha Yesu zinthu zomalizira zimene Yesu analankhura asanapite kumwamba mu mitambo zinali. *Pitani ku dziko lonse ndipo pangani anthu kukhala ophunzira anga. Phunzitsani iwo mu njira zonse. Batizani iwo mu dzina la Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera.*

Ngati ndikagona pakama mwina pafupi kufa ndipo ndili kukuuzani inu kumakutu anu mwana ndi mau omalizira ndithu ndipo mau omalizira amakhal ofunikira kwamabiri. Sichoncho? Mwa mau ena amenewa amene Yesu analankhula ndi kuti Akhale ophunzira anga abatizeni iwo. Aphunzitseni kuti amvere zonse zimene ndikuuzani ndi mau ofunika kwambiri kwa Yesu ndipo ayeneranso kukhala ofunikira kwa ifenso. Mau oti ubatizo mumau amu chigriki ndi ubatizo kuthandauza kumizidwa kumira. Pamene anthu anamva Yesu ali kulankhula sanamvetsetse. “pitani akhale ophunzira anga abatizini mu chilankhuro chawo, anamva Yesu akuti . pitani akhale ophunzira anga abatizeni iwo kumizidwa mmadzi.

Ubatizo sunali mau a chipembedzo nthawi imeneyo. Pamene timamva mau oti ubatizo tsopano timaganiza kuti ndi mau chipembedzo nthawi imeneyo. Pamene anthu amachapa nsalu amaika mmadzi ndi zobvalazo zimakhala pansu pa madzi ndi kumachapa, ndipo akamatchuka ziwiyi amazikanso pansu pa madzi ndimazitchuka anali mau amene analipo kale ndiye ubatizo sanali mau achipembedzo ndiye pamene Yesu amati pitani akhale ophunzira anga ndiye amatiuza momveka bwino pazimene iye amafuna kuti tidziwe.

Pali mafunso ambiri pa maganizo anthu ambiri pankhani imeneyi koma mau a Yesu ndi oti ndi ofunika tiyenera ngati sichoncho ndiye kuti sitili okonzeka kubatizidwa. Timaika manda anthu akufa ndi pamene timapeleka moyo wathu ndi pamene timauka ndi kuyenda mu moyo watsopano ubatizo ndi chikondwewero chopeleka moyo ndi kulandira moyo wa Yesu. kuikidwa mmanda pamodzi ndi Yesu ndipo zinthu izi ndi zofunika chifukwa Yesu anatero. Angabatizidwe ndi ndani? Ndi funso labwino. Peturo anati ubatizo ndi kulira kwa munthu olungama mtima kwa Mulungu. Mtima umene amafuna kukhala mwa kulira kwa Yesu kwa Mulungu kukhulupirira kuti Yesu ndi mwana wa Mulungu ndi kufuna kuti

machimo awo akhululukidwe ndi kuchotsedwa akhonza kubatizidwa. Munthu amene sakhulupilira Yesu salira moyo wake kwa Mulungu ndipo sanakhulupirire kuti akufuna kukhala mwa Yesu ndi mitima yawo kufikira kuthekera kwawo ndiye kuti Sali okonzeka kuti abatizidwe.

Sitingathe kumvetsetsa bwino za ubatizo ndi kusamvetsatso bwino mmene tingakhalire mwa Yesu koma kuti moyo uyenera ofuna kulondora Yesu ndi mmene tingadziwire. Tiyenera kudziwa kuti tinapachikidwa pamodzi ndi Yesu pamodzi ndi machimo anga ndi kumva kupweteka kuti tinapha mwana wa Mulungu osalakwa. Tiyenera kufuna kunena kuti, pepani, chonde tengani moyowanga Aroma 6 amanena kuti tinafa ku machimo athu tinafa naye pamodzi ndi Yesu ndi kuyenda mu moyo watsopano. Sitiyenera kukwirira munthu amene ali ndi moyo ndipo kuikidwa mmanda ndi kwa anthu akufa. ndi zoonza mu mzimu tiyenera kufuna kufa ku machimo athu ngati sichoncho ndiye kuti sitili okonzeka kubatizidwa. Timaika mmanda anthu akufa ndi pamene timapeleka moyo wathu ndi pamene timauka ndi kuyenda mu moyo watsopano ubatizo ndi chikondwewero chopeleka moyo ndi kulandira moyo wa Yesu.

Monga mwa zonse zochitika muchikristo ndi nkhani ya mtima osati zochitika kunja kwa thupi. Tikuthandauza kuti zofunika kwenikweni tiyenera kuti tikonde Yesu mwana wa Mulungu ndi kupeleka moyo wathu kwa iye. Koposa mau amene amanenedwa a zaubatizo Yesu akufuna kutipatsa ife mzimu woyera ndi kukhululukidwa machimo athu. Yesu akufuna kuti tibatizidwe ndi mzimu umodzi kulowa mu thupi limodzi akufuna kuti tikhale mu mbali ta Atate, mbali ya mwana ndi mbali ya mzimu woyera. Kodi nanga tikhathe kunena zotero monga mwa chizolowezi kuti iye akwaniritse malonjezano ake?

Yankho ndi loti simau amene timalankhura ndi mtima ndi moyo umene timapeleka kwa Mulungu umene uli ofunika. Ngati tingadziwe ndi kukhulupirira ndi mtima wathu kuti Yesu ndi mwana wa Mulungu ndi kuti Yesu anafa ndi kuti machimo athu okhululukidwa ndi kudziwa kuti tiyenera kukhala mwa Yesu osati mwa ife tokha ndiye tumumvere ndi kupeleka miyoyo yathu kuti tibatizidwe ndiye kuti tili kumwamba ndi ngati kuti mkono wa Yesu watsitsidwa kuchokera kumwamba kufikira pa ife pamene tibatizidwa. Ubatizo ndi ofunika kwambiri pali ndi malonjezo ambiri amene ananenedwa okhunzana ndi ubatizo. Satana amatsutsa ubatizo amadana nawo.

Tinaona izi India mwa chitsanzo, munthu anganene kuti ndikhonza kukhala mkristu ndipo anzake tikunena “chabwino” “chabwino” munthu oyamba anganene tifuna kubatizidwa ndipo mpaka wina amaotcha nyumba yake satana amadana ndi ubatizo zili zonse zimene satana amadana nazo, ine timazikonda.

Ubatizo ndi malo amene Mulungu amakumana ndi munthu ndi lamo opatulika. Sichinthu chimene umangochichita. Sizingakhala ndi kukhala ndi okhulupilira ena ndi zazikulu kuposa pamenepa. Mulungu ali mu ubatizo mu kupambana koposa ndi chifukwa chake Yesu ananena ma mau ake omaliza ndi chifukwanso Peturo ananena kuyamba ku mpingo yoyamba uja “Mulungu waika Yesu, uwu amene munamupha. Kukhala Ambuye ndi Kristo chifukwa anali odulidwa mtima ananena kuti inde. Tidzachita chiani amuna inu abale? Peturo mwa Mzimu Woyera adati kuti, lowani mpingo Ai. Peturo mwa mzimu woyera anati lapani chotsani machimo anu ndipo ena onse ainu lowani mmadzi ndipo mudzalandira mphamvu ya Mzimu Woyera ndi kukjulukidwa kwa machimo anu, angakhale kuti machimo anu ndi ofira adzayeletsedwa monga matalala ndipo mudzalandira Mzimu Woyera kukhala mkati mwa inu ndi lonjezo ili lili kwa inu ndi ana anu ndi kwa iwo amene ali kuti kw aiwo amene aitana padzina la Ambuye. Izi ndi zofunika ndithu ngati munthu wapeleka moyo wake kwa Yesu amamva chisoni ndi machimo ake ndipo amadziwa kuti Yesu amakhulukira machimo ndi kufuna kuti akhale mukuzindikira Yesu ndiye mafuna kubatizidwa.

Mu Machitidwe 8. Filipino anakumana ndi munthu pa njira ndipo anali waudindo wake ku Ethiopia anali wa nzeru ndi ophunzira ndithu. Anali kuwelenga mau a bukhu la Yesaya, Filipino anadza kwa iye nati, Kodi mukudziwa zimene muli kuwelenga? Anali kuwelenga za Mpulumutsi ndi Messiah, Yesu ndipo munthuyo anati ndidzadziwa bwanji ngati pali wina ondiuza? Ndipo Filipino anadza namuuza zonse za uthenga odabwitsa wa Mpulumutsi anamuuza za bwenzi lathu, ndinso Mfumu Yesu. Anamuuza za Yesu amene anali kuyenda panyanja. za Yesu amene anali kuimitsa namodwe kukhala bata. Anamuuza za Yesu amene anali kuukitsa akufa

ndi kuwonetsa akhungu kuwona. Anamuuza za Yesu amene amatenga miyoyo yosweka ndi kuyeletsanso. Ndipo pamene munthu uyu yochokera ku Ethiopia anamva mau amenewa za odabwitsa Yesu, anati siawa madzi. Batizani ine tsopano anadziwa kuti chiphunzitso cha Yesu ndi ubatizo unali olumikizidwa ndipo sanafune kuti adikire kwa kamhpindi. “Siawa madzi” chonde letsa ine ndi chiani? Anatero. Ndipo anapita kumene kunali madzi Filipino anamuuza iye kwa Yesu ndipo anabvuuka mmadzi ali ndi chimwemwe koma kufuna kwa mtima wake unali kulumikizidwa ndi Yesu mu ubatizo.

Panalinso usunga ndende ku mzinda otchedwa Filipino kumena abale athu ena anatekeredwa kunali chibvomelezi ndipo abale athuwa amasulidwa ndi mphamvu ya Mulungu. Wandende anaona kuti makomo anali otseguka ndipo anafuna kuzipha yekha. Abalewa anamuuza kuti apulumutsidwe angakhale kuti kunali pakati pa usiku, anafuna kuti abatizidwe nthawi yomweyo panali pakati pa usiku. Sikunali kotheka sikunali kophweka koma mtima wake unafunitsitsa Yesu kuti ayenera kubatizidwa kumizidwa ngati tili ndi maganizo a Mulungu pa ubatizo tikhala okondwa pa zimenezi monga mmene munthu wa ku Ethiopia wosunga ndende wa ku Filipino ndi zikwi zitali (3,000) za anthu aku Yerusalem, tsiku limodzi anali okondwa ndi ubatizo.

Tsopano pali kusiyana kotani ubatizo wa Yohane ndi ubatizo wa Yesu? Ubatizo wa Yohane unali okhulukira machimo (Mari) ndipo ubatizo wa Yesu unalinso wokhulukira uchimo (Machitidwe 2) patapita nthawi mu bukhu la Machitidwe a Paulo anakumana ndi anthu amene amafunika kuti abatizidwanso, chifukwa analandira uthenga wa ubatizo wa Yohane ndipo amafunika ubatizo wa Yesu. Choncho amafunika ubatizo wa Yesu ndiye kuti ubatizo sikungonyowa konkha ai. Anthu awa ndi ubatizo wa Yohane anali achite ntchito yabwino ndi asachimwenso. Ubatizo wa Yesu ndikubwera mu mzimu woyera wa Yesu ndi kukhala pamodzi ndi Yesu wa ku Nazarene. Ubatizo wa Yohane unali ntchito, ubatizo wa Yesu ndi wa chikhulupiriro mu mwazi wa Mpulumutsi. Ubatizo wa Yohane unali kulonjeza za kwa Mulungu ndi kumvera Mulungu ubatizo wa Yesu ndi kulira kuti tidzaziwe Yesu, ubatizo wa Yohane unali kuchita chilungamo, ubatizo wa Yesu ndi chikhulupiriro mwa Yesu kutenga machimo athu ndikusinthana ndi chilungamo ndikuchita chinthu chabwino kwa Yesu osati ntchito zimene tigwira zathu.

Atate akonde mwana wa Mulungu amene anachita pangano ndi Atate ndi kumvera iye mu zilizonse ubatizo wa Yesu ndi kulira kwathu kwa Mulungu kuti atibise ife kwa Yesu. Ichi ndi pangano lomwe Atate anachita ndi mwana linakhala pangano lathu. Osati ndi ntchito zabwino, koma chifukwa cha Yesu, uwu ndiwo uthenga wabwino, chifuwa ntchito yathu yabwino sizingathe kukondweletsa atate. Koma atate amakonda mwana ndi iye, atate amakondwera mwa iye ndiye pamene okhulupirira abisala mwa ubatizo wa Yesu, chifukwa Atate akonda mwana motero akondwera mwa iye uwu ndiwo ubatizo wa Yesu. Umene Atate anapeleka Mzimu wa mwana wake ndi kubveka ife mwana amene akondedwa uwu ndiwo uthenga wabwino.

Pali anthu amene abwera kwa ife kuti akhale mbali ya mpingo mwana sanabvikidwe mwina sanabvikidwe mwa Kristo, mwina amakhulupirira Yesu ndi mwana wa Mulungu ndi kuti ndinapeleka monga wanga kwa iye. Koma sanabatizidwe pali njira ziwiri zimene zingatsalidwe njira ina ndi ya kunja kwa thupi monga mwa lamulo ndiye kunena kuti sitingayende kuti, “tikufuna iwe ukonde Yesu, ndi kuti upeleke moyo wako kwa iye ndipo ubatizo ndiyo funika kwa Yesu. Pepani, nganzirani ndi kupemphera pa zinthu izi. awa ndiyo chiphunzitsa chochekera kwa Paulo, Petulo, Yohane ndi kwa Yesu.

Baibulo limati mu Kristo ndi amafuna mkaka wa uzimu wa mau a Mulungu monga mmene ana ang’ono khanda amafunira mkaka ndiye tinganene kuti sitingayende ndi iwe mpaka utabatizidwa? Kapena kuti tiyambe kuwapanga mau a Mulungu kuti tione ngati akukonda chakudyacho kapena ai izi zimatenga nthawi koma ngati akonda chakudyacho chimene sanamvepo ndikale lomwe. Ndiye kuti adzabatizidwa ngati sakonda mau a Mulungu sizithandauza kanthu ngati abatizidwa. Sitingayende ndi wina aliyense amene sakonda mau a Mulungu ndipo chonyezera ndi osati sakubatizidwa koma ngati akukonda mau a Mulungu.

Mu malembo woyera, ubatizo ndi chofunika ndithu kwa Mulungu ndi kwa wina aliyense amene adziwa Mulungu monga kwa munthu waku Ethiopia pamene anamva ubatizo anafuna kuti nthawi yomweyo monga anthu 3000 okhulupirira mu Machitidwe 2 mmene anamvera za ubatizo anachita ntahwi yomweyo wa ndende waku Filipo anachita nthawi yomweyo angakhale kunali pakati pa usiku sizinamukhudze kuti inali

nthawi yanji? Zinali choncho bwanji? Zinali chonchi chifukwa onse anali okonda Mulungu pamene mukonda amuna anu kapena akazi anu ndi kukufunsani zina zake zimene akufuna kuti muwapatse ngati mukonda Yesu ndiye kuti ubatizo ndi chinthu chopambana kwa iye ndiye kuti mudzakonda kubatizidwa chifukwa Yesu amakonda ubatizo.

Zimatenga ntahwi kuti mau a Mulungu afikire anthu koma tikhala tonse pamodzi ndi kulankhura zimatengera kuti ndi ubatizo ngati sadziwa ubatizo tidzakhala nawo kwa nthawi yochepa chifukwa ngati akonda mau ndi Mulungu adzakula ndipo adzabatizidwa.

Timakula mu zinthu zambiri sinchoncho? Kuyesa kwathu sikwazinthu zimene timadzidziwa kuyesedwa ndi kwa zinthu zimene zidzasinthidwe timakhala mmalo osiyana siyana kuyesedwa kwathu ndi ngati timakonda mau a Mulungu ndikuti tili kufuna kusintha nthawi zina. Kusintha ndi kobvuta ndiye tikobvuta pafunika kufatsa ndi kukondana wina ndi mzake ngati wina sakonda mau a Mulungu ndiye bvuto ndithu. Koma akonda mau a Mulungu koma zili kwa bvuta ndiye kuti tiyenera kwathandiza.

Anthu A Mulungu Ndiwo Banja

Ngati tiyenda pamodzi ngati banja tsiku ndi tsiku ndiye kuti tidzachita zonse pamodzi ngati mpingo ndi malo ongokumana pa sabata. Mmawa tili ndi bvuto chifukwa tidzaona kuti amene Sali membara wathu kapena ai. Koma ngati ndi banja tsiku ndi tsiku, koma wina sakonda mau a Mulungu ndiye kuti adzadziwika. Tidzadziwa pakukhala kwathu kwa tsiku ndi tsiku kuti ali kukonda mau a Mulungu.

Ngati munthu adzati ndabatizidwa koma sakonda akazi awo kapena amuna awo uko ndiwo kuipa ndithu. Ngati tikhala banja tsiku ndi tsiku tidzadziwa ngati ali kukonda Yesu kapena ai. Ngati tikhala banja tsiku lililonse tidzakhala ndi nthawi yolankhula za ubatizo. Sidzakhala uthenga wa ubatizo, udzakhala abwenzi kulankhura za ubatizo mwana wina sangathe kulankhura bwino za ubatizo asabweletsa wina amene angalankhule bwino za ubatizo. Pali mphatso zosiyana – siyana mu thupi la Kristo ndiye ena angalankhure bwino koposa ena. Pamene tikhala monga banja tingakwaniritse zinthu izi pamodzi tsiku lililonse. Zimasintha zinthu kukhala banja kusiyana ndi kuonelera chipembedzo chifukwa takhala ndi nthawi yosintha zinthu ndi

kudziwana wina ndi mzake. Pamene mubwera ku nyumba ya mapemphero ndiye kuti thandauzo la mpingo lili painu. Ndiye kuti tidzakhulupilira zinthu zonse panthawi yake kuti tonse tikhalepo.

Koma ngati ife ndife banja tili ndi nthawi yokambilana za kusiyana kwithu. Chifukwa timakondana osati ndi uthenga koma kulankhulana monga banja izi zimapangitsa chisangalalo ndi ufulu. Izi ndi zimene Baibulo limati mpingo ndiyo maziko a choonadi ndi, chifukwa pamodzi monga banja tikhonza kupeza maganizo a Mulungu. Pamene mphatso zikukhalira pamodzi ndikugawana moyo wathu pamodzi. Mulungu wathu adzatithandiza kudziwa maganizo ake ku zinthu zosiyana mu dera la choonadi.

Tonse Timapeza Mayankho

Izi ndi zabwino chifukwa palibe wa ife amene ali ndi maganizo abwino. Ambiri amasiyana ophunzira bwino za mbali ina ambiri Sali ku mbali ya mpingo wa moyo. Amapita ku mpingo la Mulungu mmawa basi zathera pamenepo. Sakhala ndi nthawi yoti mphatso ina isinthe moyo, ndiye ali ndi nzeru zochepe ayi akhale ndi malingaliro okhudzana ndi zophunzira zawo. Koma maganizo awo ndi osiyana ndi anzawo ndiye ali okonza ndani? Mulungu akuti maziko a choonadi ndiwo choonadi cha mpingo wa moyo. Tonse tidzapeza mayankho mu Machitidwe 15 ophunzira sanadziwe kuti okhulupirira ayenera kudulidwa kapena ai. Ndiye amabwera pamodzi kudzithetsa bvutoli. Mmodzi anati ndili kukumbukira zimene mneneri Amosi analankhura mu malemba woyera. Anali kuchitira zinthu pamodzi monga anthu a Mulungu monganso banja la Mulungu kupeza mayankho kwa Mulungu. Anachita zonse pamodzi kupeza mayankho a Mulungu popanda otchuka okhala ndi maganizo apamwamba koma linali banja la Mulungu kugwilira ntchito pamodzi ndiye Yakobo anati. Ndi chabwino kwa ife ndi mzimu woyera kuti iyi ndilo mayankho. Mpingo ndi mizati a choonadi. Tonse tikhoza kupeza mayankho. Sipofunika kukhala wa nzeru koposa kuti mukhale kuti Mulungu akugwiritsireni ntchito mu njira imeneyi.

Ubatizo Wa Yesu - Lonjezo La Tsopano

Monga ubatizo watsopano umene Yohane amaphunzitsa Machitidwe 2. limanena kuti ubatizo wa Yesu ndi kukhulukiranso machimo kusiyana kwa ubatizo wa Yesu ndi wa Yohane ndiye kuti ubatizo wa Yesu ndi ubatizo upita ku mzimu woyera ndi kuitanira kwa Messiah.

Yohane ali kubatiza Yesu asnapachikidwe pa mtanda mwazi wa Yesu usanakhetsedwe ndiye kuti Yohane anali mu chipangano chakale anali kuchita monga mwa lamulo la Alevi. Pamene anali kubatiza unali mwazi wa ng'ombe ndi mbuzi zimene zinali kukhulukira machimo ubatizo wa Yohane unatha pamene Yesu anafa pa mtanda. Yohane anadulidwatu Ambuye Yesu asanafe pa mtanda koma pano pamene Yesu ali ndi moyo ali kubatizidwa ife ndi lonjezo latsopano.

Peturo anatero mu Machitidwe 2 kuti pangago latsopano machimo anthu akhulukidwa mu ubatizo, lapani, batizani iwo wina aliyense ndipo machimo anu adzakhulukidwa ndiye mbali yopeleka moyo wathu kwa Yesu imakhudzana ndi kukhulukidwa kwa machimo athu. Koma pali chinthu china chimene Yohane sanakatha kutipatsa ife chimene Yesu anatipatsa. Yesu amatibatizanso ife ndi Mzimu woyera “ndipo mudzalandira mphatso ya mzimu woyera” mu Machitidwe 19, amuna anali kubatizidwanso kachiwiri. Paulo amawafunsa iwo ngati analandira mzimu woyera ndiye anati sitidziwa ngati mzimu woyera unapelekedwa ndipo ndi chiani? Izi ndi zimene zinapangitse kuti Paulo awabatizidwenso. Paulo anati simungabatizidwe ndi ubatizo wa Yesu osalandira mzimu woyera muyenera kukhala ndi ubatizo olakwika. Ngati mwabatizidwa ndi ubatizo wa umaphatikizanso ndi kulandira mzimu woyera. Yohane anali kubatiza ndi madzi koma Yesu adzakubatizani ndi mzimu woyera ili ndilo lonjezo la mphamvu.

Kodi ana anga adzalangidwa ndi machimo anga?

Mzimu wa Mulungu unati mu Ezekeli 18 kuti Mulungu amationa ife payenkha ndiye kuti moyo umene umachimwa ndiyo payenkha ndiye kuti moyo umene umachimwa ndiyo udzafa. Mulungu adzaweluza munthu zina ndi zoti tili ndi temberero lochokera kwa Adamu adzaweluza nyumbayo. Uku ndiye thandauzo la malembawa mu Ezekeli 18 Mulungu akuchtsa

ulemelero wake ndiye pali mtengo waukulu wopelekedwa ku nyumba yako kumachimo ako. Ana ako sadzamvera iwe ndi kukonda iwe pali kulanga pa nyumba yotere koma Ezekeli ananena kuti chilango chimene munthu amapita nacho gehena ndi la ali yense payekha payenkha.

Pali kuweluzwa kwa Mulungu chifukwa cha machimo anga amene angapangitse kuti ana anga akhale osasangalatsa. Pali tembelero la dziko lonse lapansi chifukwa cha machimo la Adamu ndi Eva. Mayi ali ndi ululu pakubereka kwawo tsopano, amuna ayenera kugwira ntchito yolemetsa kuti apeze chakudya ndi kugwira ntchito yolimba. Thaka imabereka minga ndi udzu, madzi a mu mtsinje amatipatsa ife matenda. Pali matemberero ambiri chifukwa cha kuchimwa kwa Adamu. Ngati ndili wakumva, padzakhala kuweluzwa pa banja ana anga adzakhala osakondwa chifukwa cha machimo anga umene udzapangitse kuti akhale osasangalala ndiye kuti pali kulanga ana anga adzapita ku chionongeko ndi machimo anga sadzapita ku jehena chifukwa cha machimo anga. Yesu ananena kuti pali mitundu ya nthaka zinayi. Ngati mwana wanga akonda Mulungu ndi mau ake ndi kumumvera iye. Adzapulumuka Ezekeli amanena bwino ndithu.

Ana Ndi Ubatizo

Pali nthawi pa nthawi ya umwana pamene amakhala ndi chisankho mu mtima wawo kuwulira chifukwa cha uchimo wa Adamu ndiye pamaoneka kuti ana ali ndi makhalidwe amene Sali abwino koma osati kuti Machitidwe otere adzapititsa ku jehena ai. Yesu anati mpaka mutakhala ngati mwana wang'ono sumungathe kulowa mu ufumu wa kumwamba.

Nthawi zina pamene amalozwa ana ananena kuti “ufumu wa Mulungu uli otere” ana awa sanabatizidwe. Anthu amene amabatizidwa amene amanena za machimo awo. Panalibe mbiri yonena kuti ana ali kubatizidwa. Analipo ana ambiri koma palibe zonena kuti ana anali kubatizidwa. Ndingathe kudziwa chifukwa chimene ana amafuna kuti abatizidwe koma mau woyera amanena kuti ndi okhawa amene akhulupirira kuti Yesu ndi mwana wa Mulungu. Amene moyo wawo wapelekedwa kwa Yesu ayenera kubatizidwa. Chifukwa choti Yesu anati ufumu uli monga ana awa ndiye tiyenera kukhulupilira kuti Mulungu adzateteza ana ang'ono. Analipo ana angono nthawi ya Yesu koma palibe

mbiri yoti anabatizidwa. Choncho Yesu amateteza moyo wa ana ang'ono ndipo akakula amaganiza zokhira Yesu kapena kupeleka moyo yawo kwa iye. Ndiye chisankho chiyenera kuchitika.

Chikhulupiriro cha Ayuda unali mthunzi wa chikhulupiriro cha Akristu (Ahebri 10) mu chikhulupiriro cha chiyuda padzabwera tsiku limene limatchedwa Bar Mitzuah ndi tsiku limene munthu amakhala mnyamata. Ayuda amaphunzitsa kuti anali akapolo mu nyumba ta Atate awo mpaka atafika Bar Mitzuah pakapita Bar Mitzuah pamakhala chisankho ngati adzakhala mwa Yesu kapena mwa ine ndekha. Ana a zaka zisanu sangathe kusankha. Mwana wang'ono sangathe kuti akhale mwa Yesu kapena mwa iwo wokha koma kwa ana a zaka khumi ndi khumi ndi ziwiri akhonza kusankha kukhala pa okha kapena mwa Yesu koma osati wa zisanu chifukwa saziwa kuti Yesu ndi ndani.

Mu **Machitidwe 2** limati kuti mubatizidwe muyenera kuti mulape muyenera kuti mulape kuti mubatizidwe. Simungabatizidwe ngati simungalape ndikuganiza nthawi zambiri ndi zobvuta kwa mwana wa zaka 5 (ZISANU) kuti adziwe kuti chimo ndi chiani. Mukawauza kuti anapha mwana wa Mulungu kodi adzadziwa? Sitikudziwa ngati adzadziwa? Ndi munthu yekhaya amene angadziwe kuti anapha Yesu ndi machimo ndiye angathe kubatizidwa. Yesu anati ana ali ndi Angelo amene amaima pa kupezeka kwa Mulungu Yesu mwini ndi amene analankhura ndi kuphunzitsa za izi. ndiye tiyenera kumukhulupira iye za ana athu mpaka atafika mu kukhala ndi chisankho

Kuyembekeza Pa Ambuye M'moyo Athu

September 1996, Mlowe, Africa.

(Zogawana pa nthawi yochepa pamodzi ndi abale aku Malawi)

Pamodzi!

Tiyeni tilindire tiyamike zina lake tonse pamodzi!

Anandimva ine nandimasula ku mphamvu ya mantha!

Tiyeni tiyamike zina lake tonse pamodzi kunthawi zosatha

Nonse yimbani zomuyamika ndi kumkwezeka iye.

Mnyimbo iyi ikuchokera pa Masalimo 34. Mawu onse “pamodzi” akuyimila pakatikati ka nyimboyi. “Tiyeni tiyamike dzina lake tonse pamodzi kunthawi zonka muyaya” Tilinazo zinthu zapadera dela mnyimbo yomweyi yoyamika Yehovah, kunena za Ambuye pa kumva kulira kwathu mmapemphelo, komanso ndi Angelo ake potisamalila ife kuchokera kuzoyipa zonse ndi mantha, komanso Ambuye pokwanilitsa zokhumba zathu ndi kutipatsa ife chakudya cha tsiku ndi tsiku kuchoka ku nthaka yolengedwa ndi manja ake Yehova.

Zonse tikuonazi nzapadera dala zoyikaka ndi Yehova chonse Ambuye anapeleka kw aife kuti tipindule nazo. Mwa Ambuye wathu. Ichi ndiye chofunika pa zonse.

Moyo unasanduka kuunika kwa anthu

Ndi ganizo loyikika kwa aliyense kuti tiyenera kuyembekezera pa Ambuye kudziwa kukhala mmsinkhano ya oyela mtima a Mulungu. Ndikufunafuna nkhope ya Ambuye ndi kudziwa cholinga chaka. Ichi ndiye cholinga chake. Komabe ndikukhulupirila kuti nthawi zambiri ife sitiyembekezela pa Ambuye pa zimene timafuna kuchita mmisonkhano yathu; Mmalo mwake

timamdalira Ambuye pa zokhazokha timafuna kuna kuti achite miyoyo yathu. Zinthu zambiri zimene zaphunzitsidwa kuti oyela akakhala pamodzi nkubwela ku nthawi za nthawi. Ndipo oyelawo amayenda pamodzi ndi kulingalila pamodzi. Pakakhala palibe kuyendeledwa ndi Yehova.

Ndipo oyela pamodzi tiyenda pachimene chachitika mnthawiyo tonse pamodzi. Pamene Ambuye apanga ubale wathu tonse pamodzi mwakuya. Iye amabweretsa ziphunzitso zake kuchokera kumwamba. Nthawi zina amaphunzitsa kupyolera mzopweteka ndi mukulephera kwa moyo uno. Nthawi zinanzo zimabwela mukupyolera mu chigonjetso, nthawi zinanso mzodabwitsa zake zimene amazigwiritsa ntchito potidabwitsa ife. Komanso zinthu zonsezi zimachitika pa moyo wathu wa tsiku ndi tsiku. Pamene ife tiyembekezera pa Ambuye mmoyo wa tsiku ndi tsiku tonse pamodzi mwa Ambuye.

Timalankhulana wina ndi nzake mmoyo uno wa tsiku ndi tsiku zokhuzana ndi Yesu mmoyo uno. Komanso ndikuthandizana mavuto athu pamodzi ndikuphunzira za iye nthawi zonse. Timagwilizana manja wina ndi nzake tikafooka. Chifukwa chake miyoyo yathu ngokonzeka komanso kuyembekeza pa Ambuye wathu. Zitha kuchitika kuti onse oyera akhala pamodzi, wina ayenera kuti ndiri ndi vuto, pamene wina avulala mapezanso chisangalalo cha Ambuye mkupilira kwache. Pamene oyela mtima akhala pamodzi pamenepo mlongo kapena mbale angathe kulankhula ndi kugawana chimene aphunzira ndi anza. Mungathe kuona kuti chiphunzitsochi sichikusimikizira pa kulindira pakha ayi ndi kufunsila chochita; ngakhale zotelezi zikhoza kuchitika koma zichokera kwa Ambuye pakuyembekezera pa iye. M'ubale wathu wa tsiku ndi tsiku, pakulemekeza Mulungu ndi zinthu zochepe mu miyoyo yathu, ndi kukwezana wina ndi nzake manja athu pothandizana wina ndi mzache. Kupyolera mmoyo wa tsiku ndi tsiku chiphunzitso mmawa uno pamene ndi kuyendabe mmbali mwanjira ndi m'bale kapena mlongo, pamene tikuseka or kulira pamodzi kapena zinthu zotelezi zimabwera pakulingalira kwathu.

Ndi Chimodzimidzi Lero

M'bukhu la Yohane 1. Linena za Yesu kuti moyo unasanuka kuwala kwa pa anthu ena kuona kuchokera m'moyo otisogolera. Ndi chimodzimidzi

lero. Pamene tikhala miyoyo yathu mwa Yesu ndi kuthandizana mnjira yoyenera kwa wina ndi nzake ndi mtima wathu onse. Koma makamaka tiyembekezera pa Ambuye ndi moyo wathu onse. Kusonkhana kwathu kumakhala chiyanjano cha wina aliyense pokondana wina ndi nzake. Kuphunzitsa kozama mmoyoyo yathu ndipo tayenera kukhala okhuzidwa ndi zotelozi. Mwa kukhala nacho chifundo. Pamenepo ndipamene tikhoza kusawana tonse pamodzi.

Zinthu izi nzofunikira kwambiri kugawana tonse. Pamodzi chifukwa ambiri a ife tiri ndi maganizo oti chiyanjano ndiye potheka pa zonse mmoyo wathu onse wa chikhristu. Kodi Yesu anali ndi chiyanjano ndi ophunzira ake sabata lili lonse? Osati lachiwiri lina lililonse usikuku? Ndi la Mulungu mmawa lina lililonse mmawa mawa sana chite chonchi. Mpaka na lero sachitabe. Ndi chimodzi modzi lero mpaka na kalekale. Amaphunzitsa ife pamene tidzuka natenga step oamene tiyenda komanso pamene tilingalila. Kusonkhana kumakhala pamene banja lili lonse pamodzi kuimilira, kukhala panso ndi kuyenda pa njira. PAMODZI moyo unakhala kuwala kwa dziko lapansi ndi chifukwa chake pali kufunika kuti tione wina ndi nzake ndi kukondana kunja kwa "misonkhano" Timataya nthawi pa moyo owonana wina ndi nzake mu 1 Akorinto 11, mtumwi Paulo anati ngati sitingakondane ndi kunyamulana mapewa wofooka tsiku ndi tsiku ndiye kuti misonkhano imakhala wophana osati yabwino. Tiyeni tisankhe tokha mu miyoyo yathu osati mu msonkhano kapena chiphunzitso, ikhale kuunika kwa anthu.

Tifunse Atate Pamodzi

Ndinu atate okondeka, choonde lolani kuti timve ku zinthu zimene zili zoonza osati zimene Satana amabweletsa ku makutu athu ndi mitima yathu. Satana ndiye tate wa mabodza ndipo amafuna kuti adzinamabe kwa ife kutiuzza zonama. Tikudziwa kuti mdani wathu ndi onama ndiponso ndi wakupha amafuna njira yotiphera ife koma timadziwa kuti mumatikonda ndipo mukufuna kutipatsa zinthu zabwino kuti zitimasule ife ku nsinga. Tikufunsani Inu Atate kuti mutipatse maso amene angathe kuona zonama. Tikudziwa kuti tidzakwanitsa chifukwa muli kumbali yathu. Zikomo chifukwa cha lonjezoli zikomo chifukwa cha

chiyembekezo sichidzakhumudwitsa ife. Timakhulupilira inu ndipo simudzatichititsa manyazi sitidzafa ndi mphamvu ya Yesu ndi mfumu wosatha mumafuna kuti mvula igwe ndi kuti nthaka ibale zokolora. Mumafuna kuti mitambo ibweletse dangalira pamene dzuwa liwomba mumafunanso kuti mitsinje iyende bwino kutinso ilimbe ndikupangitsa ife kudwala mumakonzanso kuti ana athu onse akule bwino ndi kukalamba ndi kuti za manja ahu zikhale zopambana kapena zolephera mumakonzanso ngati zolankhula zathu zibweletse chimwemwe kapena kukwiyitsa ena. Mumakonzanso kuti mukhale Mtendere kapena mphamvu mu mtima wanga kapena zokwiya kapenanso zolephera. Ndinu nokha amene mumakhululuka machimo anga ndi kutibweletsa kunjira yabwino uthenga wabwino ndi oti mumatikonda kwambiri pamene muli mfumu yamuyaya ndi zonse zili pansu pa ulamuliro wanu ndi uthenga wabwino kwa ife kuti ndinu odzadza ndi chifundo ndi kukoma mtima. Mfumu ya muyaya. Inde komanso bwenzi lokongolqa ndi lokondeka. Zikomo chifukwa chokhala bwenzi lathu. Mudzatitengera ife ku mbali ina ya chigonjetso....

Dzina lanu likule.

Mzimu Wotengeka Tengeka

September 1996, Mzuzu, Africa.

Malingaliro amene m'bale adagawana ndi oyera mtima mmawa wa tsiku lina pamene tidali pamodzi ku Africa.

Nditangotsegula maso anga mmawa walero. Ine ndidatsegula Baibulo langanso. Ndime yoyamba imene maso anga adaona idali ndi mau okhudzana ndi mnthunzi wa imfa, chimodzimodzi monga Masalimo 23:1 sindikadaganiza kuti ndionetsera ichi kwa inu, kupatula poti ena mwamau amenewo adali ofanana, ndipo mau oyambirira eni eniwo maso anga adaona mmawa uno adandibweretsera chikondwerero.

Kukhala Pamene Mthunzi Siungatikhudze ife

“Ngakhalebe, sipadzakhalanso zowona kwa iwo amene akhala ali m'mavuto.”

Mulungu adzachotsa zonse za zowawa ndi mavuto athu. Iye adzatsuka chikayiko chathu. Ili ndilo lonjezano lake. *“Anthu akuyenda mumdimawona kuwala kwakukulu. Pa iwo akukhala mudziko la chigwa chanthunzi wa infa, kuunika kwakukulu kwaoneka.”* (Yesaya 9:1-2).

Ndime iyi imapitirira kuyankhula za m'mene Mulungu adzakulitsire mitima yathu. Iye adzachelukitsa chimwemwe chathu. Iye adzatipanga ife kuti tisangalare ngati anthu akusangalalira zokolola. Iye adzatuta zothodwa zimene zili pa ife. Iye adzachotsa chitonzo zhakugonjetsedwa kwathu. Ndipo apa pali m'mene iye adzapangire, *“pakuti kwa ife Mwana wamwamuna wapatsidwa, ndipo ulamuliro uzakhala pa phewa pache, ndipo adzamucha dzina lace wodabwitsa, wauphungu, Mulungu wamphamvu, Atate wosatha, kalonga wa Mtendere.”* (Yesaya 9:6-7)

Ulamuliro wace ndi za Mtendere sizidzatha. Pa mpandowacifumu wa Davide, ndi pa ufumu wace, kuukhazikitsa, ndi kuucirikiriza ndi ciweluzo ndi cilungzmo kuyambira tsopano ndi ka nthawi zonse. Changu cha Yehova wa makamu cidzacita zimenezi.

Dzina lake ndi Yesu: Immanueli, Mulungu ali nafe. Yesu adzabweretsa chimwemwe chachikulu. Iye adzatsuka zowawa ndipo kuunika kudzafika m'mitima mwathu. Mtima ndi malingaliro ndi mphamvu za Mulungu wamphamvu. Zonse adzakwaniritsa ichi. Anthu akuyenda mumdimba (amenewo ndi fe) adzaona kuunika kwakukulu. Mlangizi wodabwitsa iye adzatithandiza ife mumayesero athu onse. Pamene tiyenda muchigwa cha mthunzi wa imfa, ife timvetsetsa kuti mthunzi siungatipweteke ife. Ndi mthunzi wa imfa chabe. Kodi mukudziwa chimene chimathamangitsa mthunzi? Kuunika kwakukulu kudzathamangitsa mthunzi uliwonse. Yesu, M'busa wathu wabwino, adzathamangitsa mithunzi yonse ya imfa m'miyoyo yathu. Nthawi zina ife timayesayesa kufufuza yankho kuchoka mmitu yathu, pamene chimene tikufunika kwenikweni kuti ife tipange ndi kutembenuza nkhope zathu kwa Yesu. Iye adzatimva kulira kwa mitima yathu ndipo adzaonjeza chimwemwe chathu, kubweretsa kuunika kwakukulu ku mitima yathu. Kwa ife mwana watibadwira, mwana wapatsidwa ndi adzatithandiza ife ngati titembenezira nkhope zathu kwa iye.

“Nchachikulu bwanji chikondi cha Atate chimene chidagwera pa ife, kuti ife titchedwe ana a Mulungu, pakuti ichi ndicho chimene tili! Ife tikhonza opanda nthumazi ndipo opanda manyazi pamaso pake pa kubwera kwake.” (1 Yohane 3:1,2:28) mu chiyankhulo cha chi Greek, chimanena kuti “Taonani ichi ndipo dabwani zachikondi chodabwitsa chimene Mulungu ali nacho pa ife. ichi ndi chionetsero cha “kutsegula maso athu ndi kuona mmene ukulu wa chikondi chake ulili.

Pali nyimbo yina imene nthawi zina timayimba. Imayankhula za mmene tiliri oposa agonjetsi.

Ife tili anthu a Mulungu, otchedwa ndi dzina lake.

Oyitanidwa kuchokera kumdimba ndi

omasulidwa kuchoka kumnyozo

Fuko limodzi loyera – oyera mtima aliyense.

Chifukwa cha Mwazi wa Khristu, Yesu Mwana

Ndi milomo yathu tiyeni tiyimbe kuvomereza kumodzi.

Ndi mitima yathu tigwire choonadi chimodzi chokha.

Pakuti iye wafafaniza machimo athu

Watilanda ife ndipo watitcha ife ake.

Ake omwe enieni.

Timveni ife, mizimu ya kumidima

Tsono inu mudzadzidwa pamene tiyima

Ife tili anthu ake, ogulidwa ndi zipyera

Ogulira ndi mwazi wa mwana wa Nkosa.

Mwaza wa Mwana wa Nkhosa

Ichi ndi chifukwa chake pali chiyembekezo chachikulu pa tonse a ife. Ichi ndi chifukwa satana adzalephera, ndipo ichi ndichifukwa chake tili oposa agonjetsi: ***ife tidagulidwa ndi mwazi wa Mwana wa Nkhosa!*** Tsono ndi mitima yathu tiyimbe chivomerezo chimodzi. Ife tigwiritse ku choonadi chimodzi chokha. Chifukwa Yesu wathu wagonjetsa tchimo ndipo wagonjetsa imfa, satana ali ngati galu opanda mano. Yesu watikonda ife ndipo watipanga ife Ake, Ake enieni.

Nthawi zina tiyenera kudzikumbutsa tokha za choonadi ichi. Ndi chovuta kukhala ndi tsiku pamene ife tikumbuka zinthu izi. ife tili opsa agonjetsi kudzera mwa mwana wa chikondi cha Atate.

Kutengeka ndi Zochitika

Pali njira yomutsatira Yesu imene ili yokhazikika pa momvedwe a matupi athu. Pamene mamvekedwe a matupi athu ali bwino, ife timamkonda Yesu, ife timasangalala, ndipo ife timayimba. Koma pamene ife sitimva bwino, ife sitiyimba nyimbo ndipo sitimpembedza iye. Ine ndikuganiza kuti anthu ambiri apamanga mu ubwino. Iwo amakhala ali ndi cholinga chabwino. Koma pali njira yomtsatira Yesu imene ili yamphamvu kwambiri ndipo imene siyiyelekezera kukhala yauzimu. Palinso njira ina imene ili yosakhudzikika. Ine sindikuthandauza chilichonse choipa. Ine ndingoganiza kuti nthawi zina ife sitimvetsetsa njira yeniyeni yomtsatira Yesu. Njira yeniyeni siyiyendera mmene ife tikumvera matupi mwathu.

Pamene ife tikuyankhula za uzimu oyendera mamvekedwe amthupi, ife sitikutanthauza kuti wina ali ndi malingaliro oyipa kapena zolinga zoyipa. Mwina iwo sadaone nkhope ya Yesu munjira yamphamvu imene iwo tsiku lina adzayiona.

Moyo Wa Yobu

Ife tawerenga kuti Yobu adali munthu olungama kwambiri pa dziko lonse lapansi. Kuchokera mwa anthu mazikwi ndi ngakhale miyanda, Yobu adakonda Mulungu koposa wina aliyense wa anthuwa. Yobu adamvera Mulungu koposaonse mwa anthu apadziko lapansi, ndipo komabe padali njira yokuya imene iye sadamudziwire Mulungube.

Padali zinthu zambiri zoipa zimene zidamuchitikira Yobu. Iye adali ndi kuwawa mtima kwambiri ndi kuwawa kwambiri. Thanzi lake lidapitiratu. Ana ake apamwamba adafa, Chuma chake chidatengedwa.

Mkazi wake adamuza kuti atukwane Mulungu ndipo afe. Iye adasiya osapitiriza kumkakamiza kutero. Ndipo tsono mtima wa Yobu udasweka kudzamuyendera iye, ndipo ndikhulupirira iye anthu amenewo amamkondadi Yobu. Iwo adasiya mabanja awo ndipo adakhala ndi Yobu kwamasiku asanu ndi awiri mu chete watunthu. Ndikhulupirira kuti iwo amamkonda Yobu ndipo iwo amatanthauza ubwino. Koma iwo sadamudziwe Mulungu bwino lomwe. Iwo adanena zodabwitsa zambiri, zinthu za uzimu kwa Yobu zokhudza mmene munthu wabwino amapezera zinthu zabwino nthawi zonse. Yobu adadziwa izi sizidali zoon. Iye adaonapo zoyipa zikuchitika kwa anthu abwino ndipo zabwino zikuchitika kwa anthu oyipa. Tsono iye sadadzilandire zinthu zimene anzake amanena kwa iye.

Munjira imodzi Yobu adali ndi uzimu oyendera mamvekedwe a thupi chifukwa iye sadalora Mulungu kupanga ntchito yakuya mu mtima mwake. Iye adali okondwa kwambiri ndi mmene amamudziwira Mulungu. Iye adadziyesa yekha munthu wabwino kwambiri. Chifukwa iye adali chifupi ndi Mulungu kuposa munthu wina aliyense, iye amaganiza kuti ali chifupi kwambiri ndi Mulungu. Iye sadazindikire kuti tsamba la udzu liri pafupi ndi dzuwa kuposa nyererere. Mtengo uli pafupi ndi dzuwa kuposa tsamba la udzu. Komabe mtengo ulibe kutali kwambiri ndi dzuwa. Mtengo ndi wautali

kuposa tsamba la udzu, komabe ukadalibe waung'ono kwambiri. Yobu sadamvetsetse phunziro ili. Iye adadziwa kuti iye adali chifupi ndi Mulungu maganizo a mmene iye adaliri kutali ndi Mulungube. Mtima wake sudali osweka za m'mene iye adaliri kutali ndi Mulungu. Chidatengera kuwawa kwakukulu kumeneku ndi kuonongeka kwa zinthu zonse za Yobu, munthu olungama kwambiri pa onse apadziko lapansi, kuti amvetsetse zinthu izi... .. atatha kudutsa mzowawa zimenezi, iye adati. *“makutu anga amva za inu, koma tsopano ine ndikhonza kuona chimene inu muli chenicheni.”* (Yobu 42:5) Yobu, munjira zina adali wa uzimu oyendera mamvekedwe athupi. Yobu amapanga izi muubwino ndipo iye adali munthu wabwino. Iye sadali kunamizira kapena kuyesezera koma iye adali kutali ndi chimene Mulungu ali chenicheni.

Ngati Yobu adali wa uzimu oyendera mamvekedwe a thupi, ine ndikhonza kunena kuti tonse aife tilinso chincho. Ndi zoon ndi anthu ena amene amangomizira ukhristu. Iwo amangoyesezera chabe. Iwo amapanga nkhope zawo zioneke za uzimu. Iwo amafuna kusangalatsa anthu awaone iwo akukonda Mulungu. Koma ife kodi, mukupusa kwithu ndi kusatetezedwa kwithu ndi kunyada ndiponso kusakhwima kwithu, nthawi zina sitigweramo mu zinthu zonga zimenezi? Ichi ndicho uzimu uyendera mamvekedwe athupi. Koma pali njira yeniyeni yamukondera Yesu imene imabwera kuchokera mkudzichepesa kwakukulu, ndipo ilibe nazo ntchito kapena kusamala ngati wina akuyang'ana kapena ayi. Imachokera mu mtima. Uzimu weniweni umachokera kukusweka mtima pamaso pa Mulungu. Imachokera mu kugwa m'chikondi ndi Mulungu amene amakhululukira machimo athu. Mwina chinthu chenicheni chikhala ndi maonetsera a pankhope nachonso! Koma chimachokera mukusweka mtima osati kuchokera mmkudzionetsera. Njira yabwino yothanirana ndi uzimu oyendera mamvekedwe a thupi kuchokera mmitima yathu ndi kudzichepetsa ife tokha pamaso pa Mulungu ndi kumufunsa iye kuti atiphunzitse ife. Kumufunsa iye kuti sule ife ndi moto, kuti ife tikhonza kulira ngati Yobu, *“ngakhale inu mwandilasa ine, ine ndidzakhulupirira inu!”*

Vuto la uzimu oyendera mamvekedwe a thupi sioti kuti tikungoyesezera kwenikweni, koma kuti ife sitidadziwebe ntchito yakuya imene Mulungu agwira mmitima yathu, monga iye afunira. Ndi chifunika kuti ife tisaweruzane wina ndi mnzake, koma koposa kuti ife tithandizane

wina ndi mnzake, koma koposa kuti ife tithandizane wina ndi mnzake kudziwa Mulungu oona. Ife tidziyike tokha pamaso pa Mulungu oona ndi kusiya iye atiotche ndi moto wake monga njira yomwe adachitira ndi Yobu. Padzakhala tsiku lakukondwa ngati ife tidziyika tokha pamaso pa Mulungu ndi kusiya iye awotche ife. Padzabwera tsiku la kukondwa ndi mphamvu. Ili lidzakhala tsiku lenileni kuchokera mkati mwakuya – osati kuti tisangalatse wina aliyense kapena kuti tidzipanga tokha kumva bwino, koma chifukwa ife taona nkhope ya Mulungu ndi mzimu wathu.

Mpingo ndi gulu la anthu amene amayenda dzanja ndi dzanja wina ndi mnzake mu chigonjetso ndi muzawawa kuti athandizane wina ndi mnzake kukhala enieni. Ndizoonza mtengo uli chifupi ndi dzuwa kuposa tsamba la udzu, koma tilibe ndi ntunda waukulu ati tiyende. Mulungu adati kwa Yobu, “Kodi udali kuti pamene ine ndinkayika madziko a dziko lapansi? Kodi udali kuti pamene ndinkalamula nyanja m’mene zingapitile muukulu wake? Kodi udali kuti pamene ine ndinkalamulira kutuluka ndi kulowa kwa dzuwa? Kodi udali kuti pamene ndinkapereka kwa nyenyezi iliyonse ya mlengalenga dzina? Ndipo kodi ukuganiza kuti iwe umadziwa mmene ungandipembere ine? Ndipo iwe uganiza kuti dzuwa kundimvera ine? Khala chete: ine ndikuphunzitsa iwe.” Ngati ife tili ndi mtima umene udzazipereka kumoto wa Mulungu, iye adzaphunzitsa ife kudziwa, iye mu mtima wake. Ichi chimabwera ndi zowawa koma ndi chabwino kwambiri. Kodi aliyense akhonza kuyenda ulendo ndi ife?

Funso

Tsono, kodi mmapanga chiyani pamene pali nyengo patsogolo pa inu imene inu mumaona china chake chimene mumadziwa chiyenera kukhala munjira ina yake, koma chilichonse mkati mwanu chikukuwa, “ichi sichili choncho!” kodi inu mumasintha mtima wanu ndi malingaliro anu bwanji kuti mukhale munzere umodzi ndi chimene mudziwacho? Mtima wanu ndi mamvekedwe athupi lanu ali njira imodzi, koma inu mukudziwa kuti ichi sinjira imene chiyenera kukhalira. Kodi inu mumalimbana nacho bwanji ndi chikhulupiriro kuti chisintho?

Kodi alipo wina aliyense amene adaonapo nkondo iyi mkati mwake? Paulo adati kwa Agalatiya kuti mzimu ndi thupi zimenyana nkondo

wina ndi mnzake. Ife tiyenera kuyembekezera kuti pazakhala nkondo mu mitima ndi malingaliro athu. Tsiku limeneli silidzabwera pamene pali nkondo mu mitima ndi malingaliro athu. Koma Mulungu wapereka kwa ife zida za uzimu kuti togwetse zimphamvu izi. Mulungu siamapanga adani kuti athawe. Adani Mulungu amatulutsa anthu aku Iguputo kudzera mchipululu kupita ku dziko la malonjezano, padali zimphona ndi zida m’dzikolo. Kodi ichi chikumveka ngati malo a malonjezano? Kodi ichi chikumveka ngati malo osangalatsa kukhalamo----- ndi zimphona zazikulu zamkwiyo? Koma ichi chinthu cha padera chimene Mulungu anachita. Iye amalibweretsa mu dziko lamkaka ndi uchi limene liri ndi zimphona zambiri. Kudabwitsa kw’amalo amene Mulungu afuna atipatse ife, chimodzimodzi ukulu ndi ukali wa zimphona za mkatimo. Mulungu amapanga ichi ndi cholinga. Iye amapanga ichi kuti atipanga ichi ndi cholinga. Iye amapanga ichi kuti atipange ife tikhale olimba. Chifukwa iye ali ndi zinthu zapadera zotipatsa ife, iyenso amalipa ife zimphona zazikulu kuti zilimbane nafe.

Mu Yakobo 1, mmanena kuti Mulungu iye yekha amapereka mayesero kuti ife tikhonze kukula mu kupirira ndi mphamvu. Ngati ife tikula mu mphamvu kenaka tikula mu kukhwima ndi ntunthu.

Yakobo 1:2–8: “muchiyese cimwemwe cokha abale anga m’mene mukugwa mumayesero a mitundu mitundu; pozindikira kuti ciyesedwe ca cikhulupiriro canu cicita cipiriro. Koma cipiriro cikhale nayo ntchito yao ndi opanda cirema. Osasowa kanthu konse.

Koma wina wa inu ikamsowa nzeru apemphe kwa Mulungu amene apatsa kwa onse modzala manja, niwosatonza. Ndipo adzamupatsa iye. Koma apemphe ndi chikhulupiriro wosakayika konse. Pakuti wokayikakayo afanana ndi pfunde la nyanja lotengeka ndi mphepo ndi kuwinduka nayo. Pakuti asayese munthu uyu kuti adzalandira kanthu kwa Ambuye; munthu wa mitima iwiri akhala wosinkhasinkha pa njira zace zonse.

Mu vesi yachiwiri ikunena kuti, “chiyeseni chachikondwerero kuti mukuyesedwa.” Ichi ndi chinsisi cha mphamvu zazikulu za Mzimu Oyera. Ngati mufuna kuona mphamvu za Mulungu mmoyo wanu, muyenera kusankha muchikondwerero pamene zovuta zibwera. Muli ndi chisankho pamene chimphona chidza kwa inu ndi lupanga lalikulu. Inu mukhonza,

monga okazonda khumi aja, kunena, “ine ndimadana ndi zimphona ndipo ndili ndi mantha.” Kapena, ngati Yoswa ndi Kalebi mukhonza kunena “Zikomo chifukwa cha zimphona.”

Mulungu wathu adzatipulumutsa ku ziphona. Pamene izo zidzabwera ku moyo wanu ndi kutsutsana ndi inu, inu mukhonza kukhala ndi maganizo oyipandimantha kapena mkwiyo, kapena, inu mukhonza kutengalupanga la Mzimu, kuthokoza Mulungu chifukwa cha zimphona chimene chitsutsana nanu, ndipo ndikudula mutu wake. Pamene mayesero abwera, ndipo adzabweradi, chiyeseni chachikondwerero. Ndipo ngati inu mudzachiyesa chachikondwerero, mudzakula mu kupilira ndi pamene zimphona zitsutsana nanu, ngati muli ndi chimwemwe, chikhulupiriro ndi kulimbika mtima pakukumana nazo, zipangeni nokha kukhulupirira Mulungu mu mtima wanu kuti mupambane mchigonjetso mudzina la Yesu. Kenako mudzakula mu kupilira ndi chikhulupiriro. Ili ndi lamulo kuti tichiyesa chachimwemwe pamene zimphona chibwera. Ngati inu mukula mu chipiliro mudzakula mu kukhwima. Mudzakula mu ubwenzi ndi Mulungu ndi mu mphamvu ya Mzimu. Ngati mufuna kukula mu chikondi ndi mphamvu ya Mzimu ndiye muyenera kuvomereza nkondo izi.

Kuthamangira ku Nkhondo

Mulungu amabweretsa, nkondo izi kuti ife tikhonza kukhala ndi ubale ndi iye. Muli zimphona nthawi zonse mudziko la malonjezano. **Monga dzikolo liriri la padera, chimodzi modzi ukulu wa ziphona.** Abale, tengani malupanga anu. Alongo tengani malupanga anu ndi kuchiyesa chachimwemwe. Sankhani monga Davide, kuti ngati muzaona dzenje munthaka muli mkango, mudzadumphira mdzenjemo ndikupha mkangowo. Uwu ndiwo mtima wa munthu wamphamvu wa Mulungu. Kuona adani ndi kuthamangira kunkhondo. Davide adathamangira kwa Goliati. Yoswa ndi Kalebi, Mose, Davide, Yesu ndi aliyense wa munthu wa mphamvu wa Mulungu adathamangira ku nkondo. Iwo adadumphira mdzenje ndi kupha mkango. Ufumu ulowedwa mokakamiza. Yesu adanena kuti kutenga motsophola kw aufumu kudzera mukukakamiza. Mulungu amayika zimphona mu dziko lonjezano chifukwa cha ife. Ndi chabwino bwino ngati izo zili kutitsutsa ife. Khalani akondwa kukhala ndi zimphona

zomwe zikufuna kuzipha ife, chifukwa ife tidzawina. Zimphona zitipanga ife kukhala amphamvu ndi okhwima, izo zitipanga ife monga Yesu.

Davide adayenera kutsutsana nao mkango ndi chimbalangondo kuti apulumutse mwana wa nkhosa. Keneko, pamene adakumana ndi Goliyati, iye adali olimba mtima. Chifukwa Davide adali ndi nkondo yaying'ono ndi mkango ndi chimbalangondo, iye sadali owopa zimphona chotchedwa Goliati ndipo adali ndi kuthekera kuchipha icho. Davide adali nako kuthekera kupulumutsa anthu a Mulungu, chifukwa tsopano adali ndi kulimbika mtima. Ichi ndi chifukwa chake Yakobo akhonza kunena kuti chiyeseni chachimwemwe pamene mukumana ndi nkondo mu mtima ndi malingaliro anu. Pamene ubale uli ovuta kwambiri nthawi zina, pamene mayesero ali ovuta, pamene m'mimba mwathu muli mwanjala, pamene anthu adana nafe kapena atinyoza ife, pamene ife atichotsa ntchito, kapena pamene mwana afa, zonse mwa izi ndi nkondo monga mkango ndi chimbalangondo.

Pamene nkondo izi zibwera mumtima mwathu ndi malingaliro mwathu (ndipo izo zidzabwera) pamene Mulungu ayika zimphona mudziko la malonjezano pa ife, tichiyese chachimwemwe. Khalani okondwa ndi zazimphona. Zimphona izi zidzakuthandizani inu kukhala ndi chipiliro. Zimphona izi zidzakubweretserani watunthu mwa Yesu. Ngati ife tidzatenga malo athu ankhondo ndi kulimbana ndi mdani ameneyu ndi osathawa ndi kukabisala, Mulungu adzagwiritsa ntchito izi kutipanga ife kukhala a ufulu ndi mphamvu. Ife sitili a ufulu ndi mphamvu chifukwa Mulungu amachotsapo mavutowa. Ife tili a ufulu ndi mphamvu chifukwa Mulungu amatipanga ife a akulu kuposa mavutowa. Inu muyenera kudziwa izi. iyi ndi nkhani ya Yesu mkati mwa inu. Ife sitifuna ziphona kuti zithawire kutali. Ife tifuna kudumphira mdzenje ndi kudula mutu wa chiphona. Ife sitifuna Goliati kuti adzipita, tifuna iye athamangire kwa ife kuti ife timuphe iye. Ife sitikuyesa kupewa nkondo. Ife tigonjetsa pa nkondoyi chifukwa ife tikufuna kukhala monga Yesu ndi ufulu mkati, ndi mitima yamphamvu ndi chikondi chakuya.

Inu mukhonza kupanga chibwana ndi pemphero la mgwirizano. Koma ngati mitima yanu ili yachidwi pa Yesu pa nkondo, inu mudzakhala bwino bwino.

Kuonetsa pa Moyo Wa Paulo

Ife timayankhula poyamba m'mawa uno zokhudza moyo wa Paulo. Paulo adali ndi kukumana ndi Mulungu kwa padera, ndipo Mulungu adatsegula maso ake kuti aone mavumbulutso aakulu ambiri. Yesu adaoneka kwa iye ndipo adamuonetsa iye paradiso. Yesu adamuza Paulo ziphunzitsa zimene munthu sadamvepo kuyambira kale. Tsono ichi chitanthauza kuti Paulo akadakhala ndi moyo wodabwitsa sichoncho? Kodi mukuzindikira, Paulo adakhala mtumwi zaka makumi awiri asanamvetsetse ziphunzitsa za mu Akorinto achiwiri 12:8. iye adapempha Mulungu katatu kuti amuchotsere zowawa zake. Mulungu adanena china chake kwa iye chimene chovuta kuchikhulupirira. Monga anzake a Yobu atatu aja, ife tifuna kukhulupirira kuti zoipa sizichitika kwa munthu wabwino. Koma Mulungu ndi wabwino. Ndipo Paulo anati “Chotsani kuwawa kwa ine ndili oputidwa ndi mtenga wa satana.” koma Mulungu anati kwa mtumiki wake Paulo, “chifukwa ndakupatsa zinthu zodabwitsa zambiri ndiye ndiyenera kuti mkati mwa mtima wako umveululu kuti usakhale onyada ndi kunyengedwa ndi zinthu zimene zapatsidwa kwa iwe.

Paulo anali odabwa ndi zimenezi Mulungu ananena kuti chifukwa ali kuganiza kuti apemphera ndi kuti ululu wuchoka kwa iye. Mulungu Atate anati kwa Paulo kodi sukumbuka? Kutu mwana wanga anapachikidwa mu kufooka. Yesu anali ndi kuthekera kokhulukira uchimo mu dziko. Izi ndi choncho chifukwa anapachikidwa mu kufooka, osati kuti anali ndi mphamvu, koma chifukwa anali mu kufooka. Osati kuti sanali kumva kuwawa koma kuti ululu unali waukulu. Mmene Mulungu akufunira kuti ulemere wake uwonekere ndi kuwonetsedwa. Chomwechonso akufuna kuti ife tinyamule imfa mu matupi athu kuti tibweletse moyo kwa anthu ena otizungulira. Pamene Mulungu amatipatsanso mphatso zodabwitsa kuti timutumikire iye. Ayeneranso kupeleka ululu mu mtima mwathu kuti tisakhale ndi kunyada kapena kunamizidwa kuti tidziwe kuti zabwino zonse zimachokera kwa iye .

Sindife eni ake amphatso zimenezi nzeru ndi bvumbulutso sizibwera kwa ife chifukwa ndife abwino. Monga Mulungu anachita ndi Yobu ndi Paulo ndi momwemo anachitira ndi mwana wake Yesu mu Yesaya 53. Anadula miyendo yathu kuchokera pansu pathu. Atate amaononga miyendo yathu ndi kuti tikwanitse kuwelama ndi lkumupembedza iye. Amachita zimenezi

kuti atigwilitse ntchito kuti tisakhale wonyada. Pali mbali ya mtengo wake mu 2 Akorinto 12. “Paulo anati chifukwa choti zonse izi ndi za Yesu ndipo zimachititsa iye kukondwa ndiye ndidzakondwera ndi ululu wanga ndipo ndipo tidzakondwera mu kufooka.”

Sindidzakondwanso ndi uchimo koma ululu ndi wabwino chifukwa tikufuna cholinga cha Mulungu kuchokera mu mtima tiyenera kuti timve kupwetekeka mphamvu ya Mulungu imakhala ya ngwiro mu kufooka kwathu. Ngati tidzabvomeleze ululu ndi kulambira iyeyo. Mphamvu yake ya Umulungu idzagwira ntchito mw aife munjira zambiri mbiri modabwitsa. Ndiye timakweza manja athu kwa Mulungu ndi kunena monga Paulo ananena tigawana chiyanjano cha zowawa chake kuti tigawanenso mu mphamvu yakuuka kwa moyo wake. Uwu ndi uthenga wopambana siwaanthu ozikonda koma ndi wa anthu amene ali ozichepetsa pa maso a Mulungu. Ichi ndi chi kristu choona osati chongokhuzidwa chabe ndi maganizo athu.

Yesu ali kubwera kudzatitenga ife. Ndipo tsiku limeneli chimwemwe chidzadzaza miyoyo yathu koma pano tili ndi ntchito pokozekera mkwatibwi amenewu ndi ntchito yathu kukondana wina ndi mzake ndi kuthandizana kuti tonse monga mpingo tikonzekere kubwera kwache Yesu. Ndiye maonekedwe athu adzakhala monga Yesu pamene adzabwerere kwa mpingo wake tidzafanana naye. Tidzakhala mkwatibwi monga Yesu, Mkwatibwi amene ali wa mphamvu monga Yesu amene ali ndi chifundo ndi chikondi monga iye sizophweka ai. Koma kuyanganira maso pa Atate, monga Yesu anachitira. Ngati tiika maso athu pa iye Yesu tidzakhala mbali ya chikondwewero cha mfusulo wa mwana wa nkhusa ndipo chimwemwe chake chidzadza mitima yathu.

Miyoyo Yolumikizizana Ndi Kulukana

Tiyenera kutchura kuti kuli abale oyera mtima mu mizinda amene ali kupemphera chifukwa cha ufumu wa Mulungu kuti uwonenetsedwe pa dziko lino lapansi. Ndipo ali ozipeleka koposa mu moyo wa Yesu ndi mtima wawo yonse kufuna kaye ufumu. Monganso mutipemphelerenso ife komanso kwa iwo amene sanalambire mabondo awo kwa Balaa. Pemphelelaninso iwowo chifukwa alinso mbali ya ife.

Ndizofunikanso kudziwa kuti ngati palinso china chimene tingatumikire, ndi zopezeka ndi kulukana kwa miyoyo wathu pamodzi ndi moyo wathu tsiku ndi tsiku. Zinthu zimene Yesu wawonetsera kwa ife kuno ndi kwina konse ndi zopezeka mu kugwirana mapewa ndi kuthandizana wina ndi mzake. Nthawi zimene uchimo umatchutsidwa mu miyoyo yathu nthawi imene manja athu ofooka amakwezedwa mu khosi lathu ndi nthawi imene imasonyeza mmene ife tili. Ngati pali china chimene tingapeleke, chimabwera chifukwa ena ayesetsa kuthandiza ife. Choncho, pamene mukuwelenga bukhu ili la moyo wanu. Dziwani kuti simuli kuona anthu ochepa chabe kapena zana chabe koma ochulukana amene ali kuthandiza mu msinkhu wa wina ndi mzake, ndi miyoyo yathunso. Tiyeni ife tonse pamodzi tipitilire kusintha miyoyo yathu pokweza ndi kulambira ulemerero wa Mulungu. Yesu alandire ulemerero ndi matamando!

Unsembe wa Okhulupilira

Mu thupi la kristu pali ziwalo zambiri ndipo zina ndi zowonekera kuposa zina. Koma tisachite molakwa pa mphamvu ya mphatso imene ndi yosawonekera. Mu mpingo wa mu mzinda umene inu muli mudzakhala ndi anthu amene amalankhula – lankhula koposa anzawo koma musanyoze kapena kudelera mphatso imene ili mkati mwanu angakhale kuti simulankhura – lankhula. Inu ndi ena amene amalankhula lankhula muli ndi mulingo umodzi umene umathandiza iwo kuti akhale monga ali. Mwina nonse a inu simungakhale wowonekera monga ena ali. Koma mphatso yanu ndi yofunika ndipo gwilitsani ntchito zimenezi.

Mbale kapena mlongo amene ali pano mwina sangalankhule kwambiri mu msonkhano koma ine ndekha koma alipo amene mphatso yawo ndiyopambana kundipanga ine ndekha. Koma alipo amene mphatso yawo ndi yopambana kundipanga ine kukhala chimene ine ndili komanso kulimbikitsa zinthu mu moyo kuti zichitike, koposa kulankhula mau oposa 10,000. ngati sindingathe kuthandiza aliyense kuti akhale monga Yesu mu moyo wanga, ndipo ndidzanena kuti tili kuthokozza koposa kwa Yesu kuti ali kunditumizira anthu. Amene akuthandiza kuti ndikhale monga m'mene ine ndili. Ndikunena choncho chifukwa posakhala kuti ndinu ndani mungathe kuchita posintha dziko kwa Yesu. Musaganize kuti ndinu opambana pamene muli kulankhula kwambiri pa msonkhano ena

sangalankhule kwambiri koma mu njira zina ndi opambana chifukwa cha zimene ali pa miyoyo yathu zimene zili zowelengedwa kwa Mulungu.

Ndifuna kuti mudziwe m'mene wina inu anga thandizire dziko mmene mungakhale mwa Mulungu wina ndi mzake kuthandizana kuti mukhale monga Yesu. Mulungu safuna wozipambanitsa kapena otchuka. Ali kufuna anthu amene angazichepetse kwa wina ndi mzake. Mulungu akufuna anthu amene ali ndi kuthekerana kugwilitsidwa ndi iye.

Funso limafunsidwa posachedwapa

“Kukhudzana ndi zinthu zimene talankhulazi unsembe wa okhulupilira, mmene tingakhale pafupi ndi Yesu mmene mpingo uli - kodi ndife utsalira ndi madera ena? Kodi alipo ena mu maiko amene akuzidziwa zinthu izi ndi kuyenda mu zimenezi?”

Ndifuna inu kuti mudziwe udindo wanu chifukwa ndinu oyambilira kwa anthu mu dziko ndi kuti muyende mu izi. alipo ochepa onse choonadi ichi cha Mulungu. Alipo ochepa amene amazimvetsa izi m'maiko onse choonadi ichi cha Mulungu. Mulungu wakulamulilani kuti mupite ku maiko onse ndi mau ake kumalo amene ali pafupi ndi inu. Pitani ndi kulalikirira uthenga wabwino wa ufumu woyera wa Mulungu. (1 Akorinto 12, Machitidwe 2:42-47) Mulungu wakusankhani ngati apadera dera ndi uthenga wapadera uwu pang'ono ku India kapena Polande ndi kwina konse amene amadziwa zinthu izi zimene zili pamtima wa Mulungu. (Aefeso 3:10) Mulungu ali kunong'oneza zinthu izi mu makutu anu za mpingo kuti mukhale mu moyo uwu ndi peleka uthenga wotere. Kodi mudzapititsa uthengawu kwa onse? Uthenga wabwino wa ufumu uyenera kupita ku maiko onse. Pamene chionongeko chidzabwera! Ndili ndi chiyembekezo choti mudzalimbika ndi chikhulupiriro pochita izi.